

K U S

Kusintha kwa Chuma Chanu

MPHAMVU YA MPUMULO

I N T

GARY KEESEE

H I K A

Wokonedwa mwa Kristu,

Ndipemphero lathu kuti wapeza chipangizochi cha maphunziro kukhala dalitso la chilimbikitso kwa iwe! Chonde khala womasuka kugawana bukuli ndi abwenzi, apabanja ndi ziwalo za m'tchalitchi yako. Komanso utha kupita pa FLNFree.com kukatenga makope owonjezera ndi maphunziro ena aulere m'chilankhulidwe chako.

Mulungu amakukonda ndipo ali ndi dongosolo lodabwitsa la moyo wako. Kuphunzira momwe Ufumu wa Mulungu umagwirira ntchito kunasintha moyo wathu kukhala wabwino, ndipo tikukhulupirira kuti zidzateronso kwa iwe!

Ndi chiondi mwa Kristu

Gary ndi Drenda Keese



P.S. Kumbukira kupita ku *website* yethu yaulere FLNFree.com kukatenga maphunziro ena aulere m'chilankhulidwe chako!

K U S

Kusintha kwa Chuma Chanu

MPHAMVU YA MPUMULO

I N T

GARY KEESEE

H I K A

Your Financial Revolution,

The Power of Allegiance. Chichewa. By Gary Keesee

© Gary Keesee, 2023

Originally published in English

ISBN: 978-1-945930-03-4

Faith Life Now

P.O. Box 779

New Albany, OH 43054, USA

You can reach Faith Life Now Ministries on the Internet at

FaithLifeNow.com

Kusinthika kwa Chuma Chanu

Mphamvu ya Mpumulo. Chichewa. Ndi Gary Keesee

© Gary Keesee, 2023

Zosindikizidwa koyamba mu Chizungu

ISBN: 978-1-945930-03-4

Faith Life Now

P.O. Box 779

New Albany, OH 43054, USA

Mutha kufika ku Faith Life Now Ministries pa *Internet* pa

FaithLifeNow.com

Ndikufuna kupereka buku ili kwa mkazi wanga, Drenda chifukwa chakhala chilimbikitso chake, chikhumbo chake pa zinthu za Mulungu ndi chikondi chake pa banja lake komanso pa ine zomwe zandilimbikitsa m'zaka zonsezi. Pamodzi tavomereza kuti maloto amasandulikadi choona!

Gary Keesee

ZAMKATIMU

KUYAMBA	7
MUTU 1: Mpumulo-Zoyambirira.....	13
MUTU 2: Ufulu wa Ulamuliro.....	31
MUTU 3: Ufumu Ndiwo Yankho Lanu.....	55
MUTU 4: Ndinapeza Fungulo Yaikulu ya Ufumu.....	79
MUTU 5: Kuyenda pa Ndege ndi Kwabwino Kuposa Kuyenda ndi Miyendo.....	95
MUTU 6: Pali Zambiri pa Umoyo Koposa Kungolipira Ngongole.....	119
MUTU 7: Izi ndi Zosatheka!.....	135
MUTU 8: Magawo Awiri.....	149
MUTU 9: Kukhala ndi Zokwanira Koposa!.....	167
MUTU 10: Chinsinsi cha Magawo Awiri	193

KUYAMBA

Tsiku limene tinachoka ku kanyumba yakufamu linali tsiku lowawa komanso losangalatsa kwambiri. Tinali titakhala mukanyumba kakufamu kakang'ono, kothaitha kwa zaka pafupifupi zisanu ndi zinayi, ndipo tsopano ndinali nditanyamula bokosi la katundu lomalizira kupita naye ku galimoto yathu. Ndinali kupita ku nyumba yathu yatsopano yotalika kwa 7,700 *square foot*, yomwe tinamanga tokha, ku Georgia imene inali pa maekala makhumi asanu ndi mphambu zisanu a munda wokongola ku Ohio, yomwe inalinso ndi malo a maekala makumi awiri a mitengo ndi madambo. Linali loto limene linakhala lovuta kuliganizira zaka zingapo mmbuyomo.

Ngakhale kuti tinali kuchoka ku kanyumba kakufamuyi, ndimakakonda kanyumba kakaleko. Inde, ngakhale kanali ndi mazenera ake othyoka, chipinda chapansi cha dothi, komanso kumalumidwa ndi njuchi nthawi ndi nthawi koma tinapirira pamene tinali kukhala mmenemo. Zokumbukira zambiri zinabwera mmaganizo. Awiri mwa ana anga asanu anabadwiradi mmenemo mu chipinda chochezera.

Tinali ndi nthawi yambiri yabwino kumeneko komanso nthawi yambiri ya mavuto azachuma ndi opanda chiyembekezo. Panali zinthu zambiri zimene tinali kufunikira kuti tiphunzire. Ngakhale kuti ndikovuta kuganizira tsopano, pamene tinasamuka mu

kanyumba kakale kakufamuyi zaka zisanu ndi zinayi mmbuyomo, timavutika kulipira ndarama yokwanira \$300 pamwezi kwa mwini nyumba. Magalimoto athu onse awiri anali akale kwambiri, atayenda mazana mazana a mamailosi, komanso anali ndi ngongole za misonkho. Panthawi imeneyo, zinali kuoneka kuti tinali ndi ngongole kwa aliynse. Tinali ndi makhadi angongole khumi opanda ntchito ndi oletsedwa; ngongole ku ma *company* awiri azachuma; komanso, zolipira magalimoto athu awiri; ngongole ya *IRS*; zikwi zambiri zangongole zomwe tinali nazo kwa achibale athu; ndipo mndandanda umapitirira. Tinali kukhala umoyo wongopeza ndarama zofunikira, timagulitsa chilichonse chomwe tinali nacho nthawi zina kuti titha kungogula zakudya. Zinthu zomwe tinali nazo zinali zakale kwambiri komanso zosweka zomwe tinagula kalekale kwambiri.

Mavuto athu achumawa panthawiyo anali ndi chiyembekezo chochepe cha tsogolo labwino. Kunena zoono, sindinaone chiyembekezo china kuti zinthu zingasinthe. Ndinali kukonda banja langa, ndinali ndi mkazi wokongola, koma ndinali kuwakokera ku gehena lazachuma!

Ndinali kumwa mankhwala ochepetsa kupsinjika mmaganizo, kuchita mantha, ndipo mantha anamiza moyo wanga watsiku ndi tsiku. Tiyeni tingonena kuti sindinali munthu wosangalatsa kwambiri kukhala nane pafupi. Ndimagulitsa *life insurance*, kulandira malipiro a *commission*, ndipo ndinali kutali ndi kuchita bwino, kupatula kukagwera kuphomphe lazachuma. Pang'ono ndi pang'ono, tinali kulowa mngongole mpaka panalibenso njira zina zoti tingakongole. Pamenepo ndinasokonezeka mmaganizo. Kupanikizika ndi mantha zidandizinga. Ndinali kuopanso kusiya nyumba yanga, chomwe sichinali chabwino ukamalandira malipiro pa malonda a *commission*.

Mkazi wanga anali kuganiza kuti adzakhala kutali ndi mwamuna wake, ndipo mantha olera ana anayi yekha anali nawo panthawiyi. Koma ndi wolimba mu chikhulupiriro cha mphamvu ya pemphero ndipo sanataye mtima za ine. Tinapemphera pamodzi ndi kuyamba kuphunzira fundo za Ufumu wa Mulungu. Pamene tinayamba kufunafuna mayankho ndi fundo za Mulungu, chiyembekezo chinayamba kukwera mu mitima mwathu pamene tinaona chozizwitsa chimodzi pambuyo pa china pogwiritsa ntchito zimene Mulungu anatisonyeza.

Nthawi yotsimikizika idachitika usiku wina pamene Mulungu adandionetsa kuti ndiyenera kuyambitsa *company* yanga ya zachuma yakuthandiza anthu kutuluka mngongole ndikuwaphunzitsa fundo zomwe Iye amandionetsa. Panthawi imeneyo, kuyambitsa *company* yosonyeza anthu mmene angatulukire mngongole zinali kuoneka zachilendo chifukwa tinali ndi ngongole zambiri. Tinapempherera zimenezi, koma Yehova anatiuza kuti pamene tinatuluka ndi kuyamba kuphunzitsa fundo Zake, ifenso tinapeza ufulu wathu. Kuyambitsa *company* kunali kuyenda kwachikhulupiriro popeza tinalibe chidziwitso cha mmene tingachitire zimenezo, koma tidapirirabe. *Company* yo inakula, ndipo ndarama zimene inabweretsa zinachititsa banja lathu kutulukiratu mngongole mzaka ziwiri ndi theka. Ndidzalankhula zambiri za *company* yathu mu mutu wotsatira, koma pakadali pano, dziwani kuti miyoyo yathu idasintha kwambiri! Palibe njira yomwe ndingafotokozere momwe tinamvera kukhala omasuka, momwe zimamvekera kuyenda mumsika wogulitsa magalimoto ndikulipira ndarama zogulira galimoto yatsopano. Momwe zimamvekera kupanga dongosolo, kumanga, ndi kulipira nyumba yathu yatsopano. Zimene tinali kusangalala nazo zinali zoposa zimene tikanaganizira.

Inde, kanyumba kapafamuko kanali ndi zotikumbutsa zingapo. Pamene ndinapita kukatenga bokosi lomalizira mkanyumbamo, ndinadutsa mkazi wanga ataima mu chipinda chodyeramo chaching'ono. Anandiyang'ana misozi ili mmaso mwake. Iyi

**PAMENE TINAYAMBA
KUFUNAFUNA MAYANKHO
NDI FUNDO ZA MULUNGU,
CHIYEMBEKEZO
CHINAYAMBA KUKWERA
MU MITIMA MWATHU
PAMENE TINAONA
CHOZIZWITSA CHIMODZI
PAMBUYO PA CHINA
POGWIRITSA NTCHITO
ZIMENE MULUNGU
ANATISONYEZA.**

sinali misozi yachisoni; inali misozi yachisangalalo komanso misozi yamalingaliro, pamene anali kukumbukira zonse zimene Mulungu anatiphunzitsa kumeneko. Ndinadzilimbikitsanso pamene ndinayang'ana komaliza mu zipinda, pokumbukira ndi mitima iwiri zonse zimene zidachitika kumeneko. Tinali kutseka mutu wankhani wina mmiyoyo yathu ndi kupita kugawo latsopano. Ndi chiyani chinali patsogolo pathu tsopano? Ulendowu unali utatichotsa ku kupsinjika mmaganizo, opanda chiyembekezo, kupita ku

tsogolo lodzala ndi chiyembekezo. Pamene ndinapita panja ndi bokosi lotsiriza, ndinaima ndikuyang'ana mnyumba ndikumwetulira. “Ayi, sindidzakusowa. Ndili ndi malo abwinopo tsopano.”

Zoonadi chinali chosangalatsa kusamukira ku nyumba yathu yatsopano. Koma chinthu chabwino kwambiri paulendo wathu chinali chakuti pomalizira pake panali mpumulo! Ndinali kutha kuganizira za tsogolo langa osati zakungolipira ngongole basi. Kwa zaka zambiri, kukhala mu mpumulo Wake kunali loto lenileni! Kulipiridwa kwa magalimoto athu ndi mpumulo. Kukhala

wopanda ngongole ndi mpumulo. Kukhala ndi nyumba yamalo anga pa maekala makumi asanu ndi mphambu zisanu olipiridwa ndi mpumulo. Kuona kumwetulira pamaso pa mkazi wanga akamapita kokagula osadandaula za ndarama ndi mpumulo. Kukhala ndi zonse zomwe timafunikira, kukhala ndi ndarama zokwanira kuti titha kupereka zikwizikwi zandarama kwa ena ndikuthandizira Uthenga Wabwino ndi mpumulo. Koma mwina kusintha kwakukulu mmoyo wanga kunali kusadzuka ndikagona pamene tsiku ndi tsiku ndinali wopsinjika ndi mantha zomwe zidazungulira moyo wanga mzaka zonse zoyambirira. Kuthanso kulota zinthu zabwino mmalo molota kuti udzangopulumuka sabata imodzi ndi mpumulo.

Inde, tsiku lomwe ndinali kunyamula mabokosi omaliza mu galimoto kupita ku nyumba yathu yatsopano linali lowawa komanso losangalatsa. Koma ndikhulupirireni, kukoma kwa mpumulo womwe ine ndi Drenda tinapeza kudagonjetsa malingaliro owawa akusiya kumbuyo zikumbutso kotero kuti tidamvanso ngati ana aang'ono asukulu, akuseka ndikulota limodzi.

Ndikudziwa zomwe mukuganiza. Ndikufuna ndikadakhala nazo zimenezo. Ndikufuna ndikadakhala ndi zomwezo ndikuseka, kulota, ndikutha kuika maganizo pa chinachake osati kungolipira ngongole chabe. Ngakhale kuli kovuta kukhulupirira fundo imeneyi mu bukuli, ndikukutsimikizirani kuti zimene Drenda ndi ine tinapeza ndizopezekeratu kwa inu monga momwe zinaliri kwa

**INE NDI DRENDA
TINAPEZA
KUDAGONJETA
MALINGALIRO OWAWA
AKUSIYA KUMBUYO
ZIKUMBUTSO KOTERO
KUTI TIDAMVANSO
NGATI ANA AANG'ONO
ASUKULU, AKUSEKA
NDIKULOTA LIMODZI.**

ife. Pemphero langa ndikuti pamene tikugawana nkhani yathu, mudzalimbikitsidwa kuti mugwiritsenso ntchito malamulo ndi fundo za Mulungu pa moyo wanu.

Sizovuta kwenikweni; mukungofunika kupeza mphamvu yampumulo!

Idzani kuno kwa Ine, nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine nd idzakupumulitsani inu. Senzani goli langa, ndipo phunzirani kwa Ine, chifukwa ndili wofatsa ndi wodzichepetsa mtima, ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti goli langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wo pepuka.

— Mateyu 11:28-30

MUTU 1

MPUMULO - ZOYAMBIRIRA

MPUMULO - kuikidwa kapena kuthandizidwa kuti mukhale pamalo ake enieni, mphindi kapena nthawi yopumula kapena kusiya kuchita zinthu zolemetsa kapena zosowetsa mtendere. (*Google*.)

Kodi mwatopa? Kodi mumatopa masiku ambiri popanda chimene chakugwirani? Kodi kufuna kwanu ndarama kumalamulira zitsimikizo zanu za komwe mumagwira ntchito kapena momwe mumagwirira ntchito kapena nthawi imene mumagwira ntchito? Kodi zimaoneka ngati simudzatulukamo mngongole? Kodi zikuoneka kuti mukukhala umoyo wa mpikisano wopezera chuma? Ngati muli choncho, simuli nokha.

Kodi mudaonapo kathayala kamene tinyama tating'ono-ting'ono timakwerapo? Ndikukhulupirira kuti mudatero, koma ngati mulibe, ndi kathayala komwe kamaikidwa mkati mwa kakhola katinyama tating'ono-ting'ono. Tinyamato tikhoza kukwera pa thayala limenelo ndi kuthamanga ndi kuthamanga ndi kuthamanga mpaka titatopa. Koma liripo vuto limodzi lokha ndi kathayalako. Palibe kanthu kuti tinyamato timathamanga bwanji kapena kwa nthawi yaitali bwanji, tikatopa ndikutsika, timakhala pamalo omwe tidayambira. Palibe chomwe chasintha. Timatha kupukuta

thukuta patinkhope taito tating'ono taubweya ndikumva kukhut-itsidwa. Koma palibe chimene chachitidwa kuti chipindulitse mmiyoyo yaito; tikadali totsekeredwa mkhola topanda ufulu. Ichi ndichoonadi kwa anthu ambiri, mwinanso anthu oposa ambiri, ndi moyo wawo wachuma. Amagwira ntchito molimbika sabata lonse ndipo amatopa kwambiri kumapeto kwa sabata, koma Lolemba mmawa likafika, amadzapezeka ali pamalo omwewo monga analiri sabata latha. Zonse zomwe angochita ndikungopulumuka kwa sabata limodzi.

Ichi chinali chithunzi-thunzi cha moyo wanga kwa zaka zisanu ndi zinayi. Ndimagwira ntchito maola khumi ndi asanu mpaka khumi ndi mphambu zisanu ndi zitatupatsiku, ndinali wakhama, ndipo ndinagwira ntchito molimbika, koma nditatha kupereka chakhumi changa, ngongole zanga, ndi misonkho, panalibe kanthu kotsalira. Nthawi zambiri, ndinali kusowa zomwe ndinali kufuna ndipo pang'onopang'ono ndinayamba chizolowezi chobwereka kuti ndipulumukepo. Mavuto a zachuma akachulukwa, ndinali kuthamangathamanga kwambiri, koma sindinaphule kanthu. Pamene ndinaima ndi kuyang'ana zomwe zachitika, ndinali kubwererabe mmbuyo.

Izi, ndithudi, zinatsogolera kuzovuta mmaganizo. Kukhumudwa ndi mantha zomwe ndinali kulimbana nazo tsiku ndi tsiku zidakhudza maganizo anga ndi thupi langa pang'onopang'ono. Kudzidzimuka, mantha aakulu, ndi kutha mphamvu kwa ziwalo zinayamba kulowa mthupi langa pang'onopang'ono. Madokotala sanathe kudziwa chomwe chinali cholakwika mwa ine. Mantha adandizinga kwambiri moti sindinali kudziwa ngati ndidzakhala ndi moyo kapena kufa. Kugulitsa katundu wamnyumba ndi kubwereka ndarama kwa achibale kudapitirira pafupifupi zaka zisanu ndi zinayi!

Pofika nthawi imeneyo, panalibenso chinthu china choti ndigulitse, ndipo panalibenso umunthu wanga. Ndinali nditatheratu. Mukadatha kunyamulira umunthu wanga ndi chowolera marara, popanda chisangalalo chilichonse chomwe chidatsalira mmoyo.

Obwereketsa ndarama anali atachita mndandanda kuti andimangitse, ndipo ndi pamene zidachitikira. Ndikusowa chiyembekezo choti ndipume bwino, foni inalira. Foni inabwera monga zilizonse za mmawa: “Bambo Keese, monga mukudziwa, muli ndi ngongole ya munthu wathu. Kodi mukuganiza kuti mungaibweretse liti? Chabwino, Bambo Keese, munanena katatu konse nditakui-mbirani. Ngati simutipatsa ndarama mmasiku atatu akudzawa, munthu wathu adzakumangitsani pa ngongoleyi. Mwamva kodi, Bambo Keese? Masiku atatu. Tsalani bwino.”

Kundiimbira foniku kunandigunda ngati *ton* ya njerwa. Osati kuti sindinali kudziwa momwe mavuto athu azachuma analiri. Ndinalibe ndarama. Zonse zomwe ndinali nazo zinali zakale. Firiji yanga inali yopanda kanthu. Banja langa lokongola linali kugona pafupi ndi malo a moto kuti lizitenthetsedwa chifukwa kunalibe ndarama yogulira mafuta ofunditsira nyumba. Ndinalibe poti ndingagwire. Anzanga ndi achibale anali atatopa ndi kundilipirira zinthu zanga. Mosokonezeka, ndinakwera pang'onopang'ono kupita kuchipinda changa ndikugona pabedi. Ndinalira ndipo ndinafuulira Yehova kuti andithandize.

Ndiganiza kuti ndinadabwa ndi momwe Yehova analankhulira kwa ine mofulumira. Silinali liwu lomveka koma liwu limene linatuluka mwadzidzidzi mu mzimu wanga ndi mu maganizo mwanga ndi mphamvu. Chinthu choyamba chimene Ambuye ananena kwa ine chinali chakuti kusokonezeka kumene ndinali nako kunalibe chochita ndi Iye. Ndikuganiza Iye ananena zimenezo chifukwa

ndinali wosokonezeka pang'ono chifukwa Iye, mmaonedwe anga, sanatithandize. Timapita ku tchalitchi yaikulu, tinali owolowa manja pakuthandiza, ndipo tinali kupereka chakhumi chatu nthawi zambiri. Mmalo mwake, Iye anati chifukwa chimene ndinali mchisokonezo chimenechi chinali chakuti ndinali ndisanaphunzirepo mmene Ufumu Wake umayendera. Iye anandiuza kuti Ufumu Wake sugwira ntchito monga momwe dziko lapansi limagwirira ntchito pa za ndarama, ndipo ndikofunikira kuphunzira dongosolo la Ufumu Wake la kasamalidwe ka chuma ngati ndikufuna kukhala womasuka.

Ndikukumbukira ndikuthamangira pansi ndikugwira Drenda ndikumuuza kuti Ambuye anali atangolankhula nane ndipo yankho linali Ufumu Wake. Ndithudi, tinali osokonezeka pang'ono, pamene tinali kuganiza kuti tinamvetsetsa chimene Ufumu Wake unaliri. Kupatula apo, monga ndidanenera, timapita kutchalitchi yaikulu, tonse timakonda Mulungu, ndipo timadziwa kuti tili panjira yopita kumwamba. Koma pamene tinadzaunikiridwa, tinadziwadi zochepa ponena za Ufumu Wake ndi mmene unagwirira ntchito.

Ndinasangalala kwambiri kuti Mulungu analankhula nane ndiponso kuti Adandiululira yankho—Ufumu Wake. Tanthauzo lake linali lisanagwirike, koma ndinalimbikitsidwa. Choonadi chinali chakuti sindinadziwa chomwe Mulungu amatanthauza ndi liwu lakuti *ufumu*. Ndidayenera kufufuza kuti mu liwu limodzi limenelo munalidi yankho lomwe ine ndi Drenda tidakhala tili kulilakalaka ndi kulifunafuna.

Drenda ndi ine tinagwirana manja tsiku limenelo ndikupemphera. Choyamba, tinalapa kwa Mulungu chifukwa chosapeza nthawi yophunziradi Mawu Ake ndi mmene Ufumu Wake umayendera pa nkhani ya zachuma. Chachiwiri, ndinalapa kwa Drenda monga mutu wa banja chifukwa chowalowetsa mmavuto

amenewa. Tonse tinapemphera ndi kuvomereza kuti tinali otsimikiza mtima kuphunzira mmene Ufumu umagwirira ntchito ndi kukhala ndi moyo wosiyana ndi umene takhala nawo kwa zaka zisanu ndi zinayi zapitazo.

Njira yabwino yofotokozera zomwe zidachitika patsogolo pake ndikuyang'ana pa choyatsira magetsi. Lowani mchipinda chomwe kuli mdima ndikungotembenuza choyatsira. Kuwala! Mutha kuona. Umu ndi mmene zinaliri pamene Mulungu anayamba kutiphunzitsa za Ufumu wake. Zinali ngati munthu wayatsa magetsi, ndipo timatha kuona zinthu zomwe sitinazionepo. Tinayamba kumvetsa kuti Ufumu wa Mulungu ndi boma limene liri ndi malamulo osasintha. Tinazindikira kuti titha kuphunzira malamulowo ndi kugwiritsa ntchito mphamvu ndi nzeru za Mulungu kuti tipeze chuma chimene timachifuna.

Tinali okondwa kwambiri komabe osokonezekanso. Panali nkhani zochititsa chidwi kwambiri zimene zinachitika pamene Mulungu anayamba kutiphunzitsa mmene Ufumu Wake umayendera. Sindidzafotokoza zambiri za nkhani zoyambirira pano monga momwe zafotokozedwera mu buku loyamba mu mndandanda wamabukuwa, *Kusinthika Kwa Chuma Chanu: Mphamvu Yakhulupirika*. Mutha kupeza bukuli pa garykeese.com kapena pa Amazon.com. Muyeneranso kupeza buku langa, *Faith Hunt*, lomwe limakutengerani ku chiyambi kumene Mulungu adayamba kundiphunzitsa momwe ndinakololera zofunikira posaka gwape. Koma kuti tifotokoze mwachidule, ndiloreni ndikupatseni chitsanzo chimodzi pano.

Monga ndakuuzani kuti, mmaso mwathu tinali mngongole imene panalibe poithawira. Ngongole za IRS, kwa ogulitsa katundu, makhadi khumi opanda ntchito ndi oletsedwa, ndi ngongole ku

ma *company* azachuma atatu pa chiwongoladzanja cha 28%. Tinali ndi ngongole kwa dokotala wamano, ochapa zovala, makolo athu, ndi anzathu. Kwa onse amene mungatchule, tinali nawo ngongole. Mwachilengedwe, panalibe chiyembekezo. Malonda anga sanali kuyenda bwino, ngakhale kuti ndinali kugwira ntchito mwakhama. Koma tsopano poona Ufumu ukuchita zinthu zodabwitsa kwambiri (werengani nkhani mu mabuku awiri otchulidwa pamwambapa), tinalimbikitsidwa kuti Ufumu ndiwo unali yankho lathu. Sitinali kudziwa kuti tingachite bwanji, koma tinali ndi chidaliro kuti tinali panjira yoyenera.

Ndipo usiku wina Mulungu anandipatsa loto ndipo anandi-onetsa mu maloto amenewo kuti ndiyenera kusiya *company* imene ndinali kuigwirira ntchito kwa zaka zisanu ndi zinayi ndikuyamba *company* yangayanga—tsopano mvetsetsani ichi—kutidithandize anthu kutuluka mngongole! Ndikudziwa; misala, sichoncho? Ndikutanthauza, ndikadadziwa momwe ndingatulukire mngongole, ndikadatero zaka zapitazo. Koma ichi ndi chenicheni chimene Iye anachita. Ndithudi ndinadabwa pang'ono. Sindi-nadziwe konse momwe ndingayambitsire *company* yangayanga kapena zomwe zimafunikira. Koma *company* yothandiza anthu kutuluka mngongole? E-ee, ndinali kufunabe wina woti andiuze momwe ndingachitire zimenezo!

Pamene ndidayamba kupempherera ichi, ndinakumana nacho chosintha moyo ndi Mzimu Woyera mokhudzana ndi momwe izi zingachitikire. Zinachitika pamene mmodzi mwa ondigula ataimba foni yokhudza malonda anga a *insurance*. O-oo, ndinaiwala kukuuzani kuti ndinali mu *macompany* a zachuma ndikugulitsa ma *insurance* ndiponso za chitetezo pamene zonsezi zinachitika. Ndikudziwa, zili ngati *plumber* yemwe ali ndi mpopi wotaya madzi

akusamalira vuto la wina aliyense koma kunyalanyaza lake. Ngakhale kuti ndinali kulephera pang'onopang'ono pa udindo wanga wa zachuma, chidziwitso chimene ndinapeza mu chidziwitso chonse mgawo limenelo mzaka zisanu ndi zinayi zapitazo tsopano chinali chofunikira kwambiri ku zimene Mulungu anali pafupi kundisonyeza.

Nditakhala pansu ndi wondigula pamodzi ndi mkazi wake patebulo lawo la mnyumba yophikira, tinaonetsana malipoti athu a nthawi zonse, omwe anatenga chithunzithunzi cha momwe iwo analiri pa zachuma pofunsa mafunso osiyanasiyana ndikulemba chomwe timachitcha kuti *data sheet*. Ichi chimagwiritsidwa ntchito makamaka kuti adziwe kuchuluka kwa *life insurance* yomwe ayenera kukhala nayo. Pamene tinali kulemba mndandanda wa ngongole zawo, onse anakwiya ndipo mkaziyo anayamba kulira pamene anali kufotokoza mmene onse awiri anali opanda chiyembekezo. Onse anali kugwira ntchito nthawi zonse koma anali kulephera mwezi uliwonse.

Tsopano, nditakhala moyo wotero kwa zaka zisanu ndi zinayi, ndipo Mulungu atayamba kuphunzitsa ine ndi Drenda za Ufumu, mukhoza kuganizira mmene ndinamvera za iwo. Monga Drenda ndi ine, iwo anali Akristu koma osadziwa mmene Ufumu umagwirira ntchito. Panthawiyo, sindikadatha kufotokoza zambiri za Ufumu kupatulapo zina mwa zinthu zoyamba zimene Mulungu anali atati-sonyeza kale, zimene ndinawauza, ndipo, ndithudi, ndinawauza zina mwa nkhani zodabwitsa zimene tinazona zikuchitika kwa ife.

Mwachidziwikire, ndinatha kuona kuti *life insurance* siinali vuto lawo lalikulu. Ndinatha nthawi ndikufotokoza zimene Mulungu anali kundiphunzitsa ponena za Ufumu, koma ndinalakalaka chinachake chimene ndikadachita kuti ndiperekenso mayankho enieni a zandarama ponena za zochitika kwa iwo.

Ku ofesi usiku umenewo, pamene ndinali kumalizitsa tsiku langa

ndi kusanthula mulu wama *file* anga amasiku onse ndi mauthenga amene ndinafunikira kuyankha, mwadzidzidzi ndinali ndi ganizo. Bwanji ngati ndidakadutsa nkhani ya *life insurance* ndikuyang'ana kwanthawi yaitali chithunzi chonse chandarama zawo? Kodi pali chinachake chimene ndikadachita? Nanga bwanji ndikadayamba kufunafuna ndarama? Chimene ndikutanthauza pa ichi ndichakuti bwanji ndikadapeza njira zotsika mtengo zochitira zinthu zomwe anali kuchita kale? Cholinga changa chingakhale chophweka, kupeza njira zotsika mtengo zochitira zinthu zomwe anali kuchita kale ndikugwiritsanso ntchito ndarama zilizonse zomwe ndapeza pa kayendetsedwe kandarama ndi ngongole zawo. Zimamveka ngati lingaliro losavuta, koma sindimadziwa zambiri za gawo lina lililonse la zachuma kunja kwa *life insurance*. Ndipo ndiyenera kukuuzani kuti izi zimachitika *internet* isanabwere. Kufufuza komwe ndikadafuna kuchita, kukadachitika mwachikale—pafoni komanso pa ma *yellow pages*.

Ndinagwira ntchito imeneyi kwa sabata lonse popeza ndimayenera kukumananso ndi wondigulayu sabata lotsatira. Ndinadabwa ndi ndarama zomwe ndikadatha kuika padera mwezi umodzi pamene ndinatenga nthawi kuti ndiyang'anitsitse dera lililonse la zachuma. Pamene ndinamaliza, ndaramazo zidawonjezeka kufika pa madola mazanamazana pamwezi. Ndi chowerengera ndarama changa, ndinaphatikiza ngongole zawo zonse kenaka ndikuikapo ndarama zomwe ndinaika padera pamodzi ndi zimene amabwezera mwezi uliwonse. Nditangodonyora *computer button*, ndinangoyang'ana yankho lomwe linali—zaka 6.2. Yankho la zaka 6.2 linali nthawi yonse yomwe wondigulayu adakatenga kuti abwezere ngongole yake yonse, kuphatikizapo ngongole yanyumba yake, osasintha ndarama zake. Inde, munawerenga bwino, osasintha

ndarama zomwe amapeza pamwezi. Ndinadabwa kwambiri ndipo ndinatsimikiza kuti ndinalakwitsa, choncho ndinachita masamu mobwerezabwereza mpaka ndinatsimikiza kuti ndinali ndi yankho lolondola. Kodi izi zingakhale zimenezo? Chifukwa chiyani onse sanadziwe izi?

Mwachangu ndinatenga mabuku angapo a ondigula ena omwe ndinali nawo ndikusanthula mwachangu ndikupeza zotsatira zofanana. Aliyense wa iwo atha kukhala wopanda ngongole pazaka zisanu mpaka zisanu ndi ziwiri, kuphatikiza ngongole yanyumba, osasintha ndarama zomwe amapeza pamwezi. Tsopano nthawi inapita ndikadali ku ofesi ndikumalizitsa kuwonkhetsa kwanga, koma pamene ndimapita kunyumba ndinali wosangalala. Ngati zomwe ndinapeza zinali zoono, ndi kuwonkhetsa kwanga konse kunalidi momwemo, ndiye kuti ichi chinali chachikulu, chachikulu kwambiri.

Ndinali ndi chidwi chofuna kudziwa kuti wondigula angayankhe bwanji pachidziwitso chamtundu uwu. Podzakumananso, ndinaganiza zolembe manambalawo patsamba limodzi. Cholinga changa chinali kungowapatsa chiyembekezo. Panalibe choti ndidzapezapo, popeza ndimadziwa kuti mwayi wogulitsa *life insurance* sungatheke. Koma ndinadziwanso kuti angafune kumva zomwe ndapeza. Mlungu wotsatira ndinayang'ana zimene ndinawonkhetsazo ndipo ndinatsimikiza kuti ndinali wolondola.

Pamene ndinaliza belu la pakhomo, ndinachita mantha za msonkhano wathu kuti udzayenda bwanji. Nditakhala pa tebulo lawo la mnyumba yophikira, ndinawauza zomwe ndinachita sabata yonse ndi manambala awo. Ndidawaonetsa mosafulumira manambala omwe ndidalemba, ndikulongosola momwe ndidapezera ndarama zoika padera, komanso dzina la *company* ndi nambala iliyonse yomwe ingafunikire pochita zomwe ndidawaonetsa. Ndinaona

kuti anali kusangalala pamene ndarama zoikidwa padera zinali kungowonjezereka. Koma pamene ndinafika ku mapeto a kukhala opanda ngongole kotheratu muzaka 6.2, kuphatikizapo nyumba yawo, pa ndarama zimene amapeza panopa, onse awiri anayamba kulira, panthawi ino ndi chisangalalo. Anakhala pamenepo misozi ikutsika mmaso mwawo ndipo amangonena kuti anadabwa ndi zotsatira izi. Adalumpha ndikundikumbatira, ndipo tinali ndi nthawi yabwino yachikondwerero usiku umenewo.

Tinene moona mtima: Kodi *IRS* idzakuwuzani momwe mungalipire misonkho yocheperako? Kodi aku *bank* adzakuwuzani momwe mungapewere kupereka chiwongola dzanja? Ayi, dongosolo lonse linapangidwa kuti litenge ndarama zanu, osati kuziteteza. Ndinadziwa kuti zimene ndinapeza zinayenera kuphunzitsidwa banja lililonse ku America! Usiku umenewo zinandikhudza kwambiri, ndipo ndinali kufuna kuchita zomwezo kwa ondigula aliyense amene ndinakumana naye.

Kotero, pokhala ndi chidziwitso chimenecho komanso chitsimikiziro cha loto limene Mulungu anandipatsa, Drenda ndi ine tinasiya *life insurance company* kumene ndimagwira ntchito ndi kuyambitsa *company* yathuyathu, kumachita zomwe ndinachitira wondigula ameneyo. Mzaka zoyambirira zimenezo, tinali kutcha *company* yathu, “*Faith-Full Family Finances.*” Dzinali linanena momveka bwino zomwe tonsefe tinali—ngati mutamvetsa za Ufumu ndi chikhulupiriro, ndarama zanu zidzadzala. Ndikuvomereza kuti silinali dzina labwino kwambiri la *company*—yesani kunena kakhumi motsatizana—koma zidayenda. Pambuyo pake tidasintha dzinalo kukhala *Forward Financial Group*, yomwe iliri lero ndipo ikuyendabe mwamphamvu.

Kunena zoono, kwa ine ndekha, chuma chathu chinali

chosakwanirabe. Tidali ndi ngongole zoti tilipire, koma tidadziwa kuti tapeza njira yoti tichite. Pamene tinayamba *company* yathu yatsopano, tinali okondwa komanso amantha nthawi yomweyo. Tinali ndi zambiri zoti tiphunzire zokhudza kukhazikitsa ndi kayendetsedwe *kacompany*, koma vuto lalikulu lomwe tinali kukumana nalo linali momwe tingapangire ndarama. Chopinga chathu chinali chakuti tinali kuona kuti sitingathe, ndipo sitinafuno kulipiritsa anthu ndarama kuti ziwathandize kutuluka mngongole. Ichi chinali choletsa chachikulu chomwe tidakhala nacho nthawi yaitali yakuchipemph-erera ndikuunika njira zina. Posanena zambiri, Ambuye adationetsa njira yodabwitsa yokhazikitsira *company* yo ndikuiika kuti ipange ndarama popanda kulipiritsa chionjezero kwa otigula.

Kenaka, tinayenera kupeza njira yofulumizitsa powonkhetsa *data* la ondigula ndi manja zomwe ndinali kuchita. Ndinali kudziwa kuti ndimayenera kulemba *computer program* kuti ndichite zomwe timachita, koma sindinali kudziwa chilichonse chokhudza ma *computer* kapena kupeza munthu amene angathe kuchita zimenezo. Apanso, Mulungu anachita zinthu zodabwitsa. Ndinalandira foni kuchokera kwa munthu wina wakutali kwambiri ndi kwathu yemwe anamva za ife. Iye anali kufuna kuona zimene timachita, monga wotigula. Anali kukonda zimene tinali kuchita, ndipo pamene tinali kukambirana, ndinapeza kuti anali katswiri wokonzana ma *computer program* ndipo anali ndi *company* yakeyake yogwira ntchito maola ochepa chabe. Ndinalankhula naye za zosowa zathu, ndipo ananena mosangalala kwambiri kuti akufuna kutithandiza pa zimene tinali kuchita. Ndinamuuzana kuti tikungoyamba kumene *company* yathu ndipo tinalibe ndarama zolipirira ntchito imene anadziperereka, ngakhale kuti ntchito yakeyo anaichita pamtengo wotsika kwambiri. Anali kufunabe kugwira ntchitoyo ndipo anati

ndikhoza kumulipira nthawi iliyonse yomwe ndarama ilowa. Kotero ndi zimene tinachita.

Anthu anali kukonda malonda athu. Nanga akanalephera kutero bwanji? Zinali zaulere, ndipo anthu anali kukonda kupeza ndarama ndi kutuluka mngongole. Malondawa anayenda bwino kwambiri, ndipo tinatha kukhala opanda ngongole mzaka ziwiri ndi theka. Posakhalitsa tinali ndi otiimirira opitirira mazana atatu omwe adagawira dongosolo athu mu dziko lonselo. Kusiya kokha kulipira ndarama zogulira magalimoto athu, tinapitiriza kumanga ndi kulipira nyumba yamaloto athu. *Company* yathu inakula ndipo yatipangitsa kuti tithe kupereka zikwizikwi za ndarama zothandizira Uthenga Wabwino komanso kwa anthu mwa zaka zambiri.

“Dongosolo langongole,” monga timatchulira likupangidwabe lero kwaulere, patha zaka makumi atatu. *Company* yo inakula mu ntchito yake mkuyenda kwa nthawi. Tidapitilira kuyang’ana kwambiri pakuikiza ndarama munthu akapuma pantchito pambuyo pa mavuto achuma amene anachitika mu 2001 ndiponso, mavuto amu 2008 pamene anthu adatayikiridwa ndi 50% mpaka 80% ya ndarama zawo zopuma pantchito. Tinafufuza njira zotetezeka zoikizira ndarama ndipo tinayambitsa malonda athu mu 2001. Ndiri wonyadira kunena kuti pa ndarama zopitirira ma million zana limodzi zomwe timasamalira otigula, palibe ngakhale mmodzi yemwe anataya ndarama imodzi mzaka khumi ndi mphambu zisanu ndi chimodzi zapitazo za kusokonekera kwachuma mdziko lathu komanso padziko lapansi. Ndipo monga mwa dongosolo lathu, palibe malipiro, palibe malipiro ogwirira ntchito kapena malipiro amkhalapakati omwe amakhudgidwa poyambirira kapena pachaka kwa oikiza ndarama. Ngati mwatopa kuchita njuga ndi ndarama zanu zimene munalandira popuma pantchito, mutha kufunsa ku

Forward Financial Group pa 1-(800)-815-0818 kapena Forwardfinancialgroup.com kuti mudziwe zambiri.

Zodabwitsa sichoncho? Lingaliro limodzi lophweka lochokera kwa Mzimu Woyera linasintha miyoyo yathu kwamuyaya! Inde, tinayenera kutulukamo, koma Mulungu anationetsa koyenera kuyenda. “Kodi unamva bwanji, Gary, kukhala wopanda ngongole?” Mtendere! Mpumulo! Taganizirani izi. Tinachoka mu mavuto aakulu azachuma ndi kufika pakutheratu ngongole, kulipira ndarama zogulira magalimoto athu, nyumba yathu, ndi china chilichonse chimene tinafuna. Kwa zaka zisanu ndi zinayi, ndinali mkupsinjika kwakukulu mphindi iliyonse ya tsiku lililonse. Ndinalibe mpumulo. Zinalibe kanthu kuti linali tsiku lanji lamlungu, kapena ngati linali la tchuthi. Ndinalibe mtendere. Nkhani zanga zachuma zinali kundit-satira kulikonse kumene ndimapita. Ndinapirira manyazi ndi mnyozo nthawi zonse chifukwa cha mavuto athu a zachuma. Mantha anali bwenzi langa lanthawi zonse, mantha owopsa komanso mankhwala opezera tulo/mtendere (*antidepressants*) zinali mchikhalidwe changa.

Mwa kusintha konse kwachuma, komanso kukhala ndi zinthu zomwe timafuna mmalo mwake, mutha kuona kuti mwa zimenezochuma chathu chinali chipambano. Inde, pomalizira pake kukhala ndi zinthu zimene tinafuna kunali chipambano chachikulu, koma chisangalalo chenicheni chinali kuona Ufumu wa Mulungu

**LINGALIRO LIMODZI
LOPHWEKA LOCHOKERA
KWA MZIMU WOYERA
LINASINTHA MIYOYO
YATHU KWAMUYAYA!
INDE, TINAYENERA
KUTULUKAMO, KOMA
MULUNGU ANATIONETSA
KOYENERA KUYENDA.**

ukugwira ntchito. Pamene Drenda ndi ine tinali kuona ntchito ya Ufumu ikuyenda patsogolo, tinali kunena kawirikawiri kuti, “Kodi munazona zimenezo?” Monga ngati choyatsira nyali chikuyat-sidwa, zonse zimaoneka bwino mkuwala; mukhoza kuona. Kukhala mukuona mutakhala wakhungu ndi kukhala wopanda mayankho pachochitika ndi chodabwitsa. Kupeza chuma chathu chenicheni, Ufumu wa Mulungu, zinalidi zodabwitsa. Kuyesera kukuuzani momwe zinakhallira nkwapafupi—kwa nthawi yoyamba mmoyo wanga, ndinali ndi mpumulo!

Sewerolo linaima! Mmbuyomu, ngati thayala lathu litaphulika, linali kukhala vuto la maganizo akulu. “Kodi ndaramazo tizitenga kuti? Kodi pali mwayi uliwonse wogula ndi makhadi?” Koma lero, ngati pazifukwa zina galimotoyo itaphulika, nditha kungofunsa mkazi wanga kuti, “Kodi ukufuna mtundu wanji tsopano?” Palibe sewero, palibe mantha, palibe ngongole, koma mpumulo wokha. Tikhoza kukhalabe pa ntchito ndi pa cholinga chathu. Osakhalanso ndi moyo wongoti tipeze pongopulumukira, titha kukhala okhudza za MOYO!

Chifukwa chake ndinena kwa inu, Musadere nkhawa moyo wanu, chimene mudzadya ndi chimene mudzamwa; kapena thupi lanu, chimene mudzabvala. Kodi moyo suli woposa chakudya, ndi thupi loposa chovala? Yang'anani mbalame za kumwamba; kuti sizimafesa ayi, kapena sizimatema ayi, kapena sizimatutira mu nkhokwe, ndipo Atate wanu wa Kumwamba azidyetsa. Nanga inu mulibe kusiyana nazo kuziposa kodi?

— Mateyu 6:25-26

Pazaka makumi atatu ndi mphambu zisanu ndi chimodzi zapitazi, ndakhala pansu ndi anthu zikwi zambiri pa matebulo awo

mnyumba zophikira ndikukambirana zandarama zawo payekhapyekha. Ndalankhula ndi makamamu a anthu zikwi zambiri padziko lonse lapansi, ndipo chinthu chimodzi chomwe ndimapeza kulikonse komwe ndimayang'ana ndikuti aliyense akufuna mpumulo!!!! Aliyense amayembekezera kutha kwa sabata, tchuthi, kapena kupuma pantchito mwachidwi—kuima ndi kupumula.

Maphunziro angapo aposachedwa omwe ndidawerenga ndidapeza kuti pafupifupi 70% ya aku America sakonda ntchito zawo, ndipo mwa 70%, 20% sadzipereka ndipo amaganizidwa kuti amadana ndi ntchito zawo. Ndi chifukwa chiyani amapita ku chinthu chimene amadana nacho? Ndi kupsinjika kotani kopirira mkhalidwe lowawa kwambiri la tsiku ndi tsiku? Kunena mosabisa, iwo ndi akapolo. (Tonse tinali. Tinakulira mdziko limene njira yokhayo yopitira patsogolo ndi kukhala ndi ndarama zokwanira kukhala ndi zosankha. Koma kwa ambiri, izi sizili choncho.) Maloto awo opita patsogolo amazilira pang'onopang'ono ku umoyo wongopulumuka pamene akupezeka ali pantchito yopanda pake mzaka zawo za makumi atatu, makumi anayi ndipo ngakhale makumi asanu.

Kafukufuku waposachedwapa akuti 69% ya anthu a ku America alibe ndarama zosungidwa zokwana chikwi chimodzi.¹ Kupsinjika maganizo ndi kuvutika mmaganizo

**KUKHALA NDI
MOYO WAMAVUTO
A ZACHUMA...
SILINALI DONGOSOLO
LA MULUNGU
PACHİYAMBI, NDIPO
SILIRI DONGOSOLO LA
MULUNGU KWA INU
NGAKHALE LERO.**

¹ Niall McCarthy, "Survey: 69% of Americans Have Less Than \$1,000 in Savings," *Forbes*, September 23, 2016, <https://www.forbes.com/sites/niallmccarthy/2016/09/23/survey-69-of-americans-have-less-than-1000-in-savings-infographic/#30d27351ae67>.

kumene anthu ambiri akukhalamo kumasokoneza malingaliro achidziwitso ndi kufunikira kwawo. Maloto amaikidwa patali kuti akwaniritse zofunikira pompopompo ndipo kukhumudwa kopanda chiyembekezo kumatenga malo. Chisangalalo palibe.

Tsiku lina ndikukumbukira ndikulankhula ndi mbusa wina zokhudza chuma. Anandiuza kuti anali kukonda kwambiri utumiki komanso amakonda anthu, koma tsiku lililonse anali kudzuka ndi chisangalalo mpaka pamene amakumbukira mmene zachuma chake zinaliri. Adandiuza kuti zinali ngati mtambo wakuda umene umachotsa kuwala kwa dzuwa, pamene maganizo ofooketsa anapangidwa mu maganizo mwake ndi kumugwira mu ukapolo wa nzeru zongopeza kupulumuka, kusowa chiyembekezo pa zachuma, ndiponso ukapolo wopanda masomphenya.

Moyo wasinthidwa wakuyang'ana ena akupambana. Hollywood yapanga ma *billion* poonetsa pa zenera lalikulu unyinji wa anthu ena akupambana. Anthu omwe sadziona okha akupambana amapeza mphindi zochepa zothawira ku zovuta zawo ndikukhala mmaloto awo poonera anthu angwiwo akukhala moyo wabwino kwambiri pazenera lalikululo.

Masiku ano masewero amakokera *mabillion* a ndarama pachaka kuchokera kwa owonera padziko lonse lapansi. Mu 2017, NFL inabweretsa ma *billion* oposa 7.8; *Super Bowl*, pafupifupi 15.5 *billion*; ndipo limenelo ndi sewero limodzi lokha!^{2 3} Anthu amakonda kukuwa molimbikitsa gulu lawo lomwe amalikonda kuti lipambane.

Koma chimene tiyenera kumvetsetsa ndi chakuti tonsefe tinaikidwiratu ndi kulengedweratu kuti tipambane—kukhala mu nkhondo,

² Michael David Smith, "Packers' Books Show NFL teams Split \$7.8 Billion in National Revenue," NBC Sports, <http://profootballtalk.nbcsports.com/2017/07/12/packers-books-show-nfl-teams-split-7-8-billion-in-national-revenue/>.

³ Joe D'Allegro, "Super Bowl Billions: The Big Business Behind the Biggest Game of the Year," CNBC, January 22, 2017, updated February 2, 2017, <https://www.cnbc.com/2017/01/20/super-bowl-billions-the-big-business-behind-the-big-game.html>.

kukhala mmasewero, ndipo pomalizira pake tidzapambana. Kusowa chiyembekezo pazachuma ndicho chizolowezi, osati chosiyana, kwa anthu ambiri—kotero kuthawa kokha ndiko kukhala ndi moyo womwe tonse timawulota kudzera mmiyoyo ya ena. Kodi nyambo yopezera *lottery* ndi chiyani? Ndi chifukwa chiyani sewero la pa *TV* lotchedwa “*Who Wants To Be A Millionaire* linali lotchuka kwambiri?” Kodi ndi chifukwa chiani njira ya zolemeretsera zidakali yesero lero lino? Yankho? MPUMULO! Aliyense watopa ndi kuthamangathamanga, aliyense watopa kudzuka ndi kulemera kwa kupeza zakudya pakuba maloto awo. Koma kukhala ndi moyo wamavuto a zachuma si chinthu chatsopano; ndipotu, chakhala chilipo kwa nthawi yonse imene munthu wakhala padziko lapansi. Komabe, silinali dongosolo la Mulungu pachiyambi, ndipo siliri dongosolo la Mulungu kwa inu ngakhale lero.

MUTU 2

UFULU WA ULAMULIRO

Kupanda chiyembekezo—umu ndi mmene ndingafotokozere moyo wathu tisanamvetsetse kupumula. Zaka zisanu ndi zinayi ndi nthawi yaitali kuti mukhale ndi chisokoneko komanso nkhawa pa zachuma. Ndikukumbukira nthawi zambiri ndimayang’ana munda wa maekala makumi asanu ndi atatu mphambu zisanu womwe tinali kulipira \$300 pamwezi kuti tikhalepo, tinali kulephera kulipira mtengo umenewo, womwe unali mtengo wotsika kwambiri, lero ndikudzifunsa ngati ndingathe kudzakhala ndi malo ngati awa.

Mwini wakeyo anali kumanga bwalo la *golf* pamalopo ndipo anali kungofuna kuti munthu wina azikhala pamenepo, kuti aziyang’anira malowo mpaka atayamba ntchitoyo, yomwe anali kuganiza kuti idzatha patatha zaka zitanu kapena zisanu. Kanyumba kakale ka pafamupo kanaperekedwa “monga momwe kanaliri,” ndipo sakadapereka ndarama zokakonzera nthawi imeneyo. Titakayeretsa ndi kukatsuka kwambiri, kanyumba kakaleko kanali ndi ubwino wake wapadera. Cholinga chathu chinali choti tikhale kumeneko zaka zitanu kenako ndikuchoka, koma mchaka chathu chachisanu ndi chitanu tili kumeneko, tinalibe chiyembekezo chakukhala ndi chilichonse.

Mulungu atalankhula nane za Ufumu, ndi kuyamba kuphunzira ndiponso kutsatira fundo ndi malamulo a Ufumuwo, zinthu zinayamba kusintha. Pachiyambi pamene chuma chathu chinayamba kuyenda bwino, tinali okondwa ndi zopambana

zazing'ono kwambiri. Ndikukumbukira ndikugula chotsukira mbale chamkanyumba kakale kakufamuko ndipo Drenda ndi ine tinali okondwa kwambiri, makamaka iye! Ngakhale nthawi zina ndinali kuthandiza kutsuka mbale, inenso ndinali wotanganidwa ndi malonda. Pokhala ndi ana anayi kukanyumba panthawiyo, nthawi zonse Drenda anali kutsuka mbale. Titagula chotsukira mbale, ndikukumbukira ndikunena mawu monga akuti, “Kodi mungakhulupirire kuti tangopereka ndarama yogulira chotsukira mbale chatsopano?” Ndikudziwa, mukuganiza kuti, “O-oo, chodabwitsa ndi chiyani pamenepo pogula chotsukira mbale?” Chabwino, kuti mumvetse izi, mudakayenera kuyang'ana zida zina zophikira zomwe zinali mkanyumba kathu kakufamu. Chitofu ndi firigi yathu zonse zinali zobiriwira za mtundu wamapeyala ndipo zinali ndi zaka makumi awiri ndi mphambu zisanu. Choncho poyerekezera, kugula chotsukira mbale chatsopano kunali kupambana kwakukulu kwa ife.

Mmutu wapitawu, ndinafotokoza mmene Mulungu anandipatsira maloto ndi dongosolo loyambitsa malonda omwe angakhale yankho ku chisokonezo chandarama zathu. Inu mukhoza kuganiza kuti, “Ndikadakonda Mulungu akadandiuza ine china chake chonga ichi.” Nkhani yabwino ndiyakuti Iye akufuna kutero, koma zilipo zinthu zina zimene muyenera kuzidziwa zokhudza mmene Ufumu umagwirira ntchito musanapeze chithandizo chamtundu umenewu. Malangizo amene ndinalandira tsiku limenelo mmalotowo, anangochitika chifukwa cha zimene Mulungu anali kutiphunzitsa zokhudza Ufumu wake ndiponso chifukwa chotsatira chimene anatisonyeza. Ngakhale kuti ndinafotokoza za Ufumu mwatsatanetsatane mu buku langa lomalizira, ndifunikira kuliyang'ananso pamenepa kuti atipatse nsanja yogwiriramo ntchito.

Anthu amandifunsa chimene ndikutanthauza ponena za Ufumu

wa Mulungu. Sindinadziwe za Ufumu wa Mulungu ngakhale kuti ndinali Mkristu. Ndinali kudziwa kuti ndikupita kumwamba pamene ndimwalira, koma sindinali kumvetsa bwino za Ufumu wa Mulungu komanso mmene umagwirira ntchito. Kuti mumvetse fundo imeneyi, muyenera kumvetsa tanthauzo la liwu lakuti *ufumu*. Mlingaliro lenileni, limatanthauza ulamuliro wa mfumu. Ufumu wa mfumu umagwira ntchito mwa mawu a mfumu. Mawu ake amakhala lamulo limene limalamulira ulamuliro Wake ndi miyoyo ya nzika zake. Fundo ina yokhudza ufumu ndi yakuti gulu la anthu *million* imodzi silipanga ufumu. Ufumu umakhazikitsa boma lomwe liri ndi malamulo olimbikitsa kutsatira malamulo a mfumu kwa nzika iliyonse yovomerezeka ya ufumu umenewo. Lingaliro ndi lakuti Mulungu ali ndi Ufumu wokhala ndi malamulo okhazikitsidwa amene nzika iliyonse yovomerezeka ya Ufumu wake imaona ngati opanda ntchito mu Chikristu cha ambiri. Akristu ambiri amakhulupirira kuti Mulungu amasankha mapemphero amene Iye amayankha kapena amene Iye amawakondera. Amakhulupirira kuti ngati asala kudya kwa nthawi yaitali kapena kuchitira Mulungu ntchito zauzimu zambiri, ndiye kuti adzakonedwa ndi Iye. Mnzanga, muli wokonedwa kale ndi Iye.

Pamenepo, ndipo simulinso alendo ndi ogonera, komatu muli nzika zinzake za anthu a Mulungu, ndi a banja la Mulungu.

— Aefeso 2:19

Simuli nzika ya Ufumu wake wokha, koma ndinu wa mu banja Lake lenileni, mwana wamwamuna kapena wamkazi wa Mfumu. Agalatiya 4 amafotokoza momveka bwino tanthauzo la izi kwa inu ndi ine.

Koma ndinena kuti wolowa nyumba ali wakhanda, sasiyana ndi kapolo, ngakhale ali mwini zonse. Komatu ali wakumvera omsungira ndi adindo kufikira nthawi yoikika kale ndi atate wake. Koteronso, ife pamene tinali akhanda, tinali akapolo akumvera miyambo ya dziko lapansi. Koma pokwaniridwa nthawi, Mulungu anatumiza Mwana wake, wobadwa ndi mkazi, wobadwa wakumvera lamulo, kuti adzawombole iwo akumvera lamulo, kuti ife tikalandire ufulu wonse wa mwana. Ndipo popeza muli ana, Mulungu anatumiza Mzimu wa Mwana wake kuti ulowe mmitima yathu, Mzimu wofuwula kuti, “Abba, Atate.” Kotero kuti sulinso kapolo, koma mwana; koma ngati mwana, Mulungu wakupanga iwe kukhala wolowa nyumba.

— Agalatiya 4:1-7

Ndinu wolandira cholowa chonsecho monga mwana wamwamuna kapena wamkazi, ndipo muli ndi ufulu wa ulamuliro monga nzika ya Ufumu Wake! Lolani izi zikhazikike mwa mphindi

**MALINGALIRO ALIPO ABWINO,
NDIPO NDIMAKONDA KUMVA
KUKHALAPO KWA MULUNGU,
KOMA PONENA ZA NKHANI ZA
ULAMULIRO, SINDIFUNIKIRA
KUMVA KUTI NDAPULUMUTSIDWA
KUTI NDIPULUMUTSIDWE. NDI
NKHANI YA ZA ULAMULIRO.**

imodzi—muli nazo kale zonse. Palibe chimene mukusowa zonse muli nazo. Choncho lekani kupempha ndi kulira. Simungathe kupempha china chake chomwe muli nacho kale. Mulungu sasankha pokhudza amene Iye adzathandiza kapena sadzathandiza. Aliyense

amene ali mwana wamwamuna kapena wamkazi wa Mulungu ali ndi chithandizo Chake kale.

Ndiloreni ndifanizire izi pokhala nzika ya United States. Ngati ndinu nzika, ndiye kuti muli oyenera kuthandizidwa ndi boma la United States kuti likhazikitse zomwe lamulo likunena. Phindu limenelo linaphatikizidwa ndi unzika wanu. Kotero, simungasale kudya ndi kupemphera nthawi yaitali kuti mupeze chithandizo Chake; Wapereka kale kwa inu kwaulere kudzera m'zimene Yesu anachita. Choncho sangalalani. Ndinu eni ake!

Ndipo Mulungu anatiukitsa ife pamodzi ndi Kristu, natikhazika pamodzi ndi Iye mzakumwamba mwa Kristu Yesu, kuti akawonetsere mnyengo zili nkudza chuma chosayerekezeka cha chisomo chake, chosonyezedwa mkukoma mtima kwake kwa pa ife mwa Kristu Yesu.

— Aefeso 2:6-7

Mawu akuti, “*natikhazika pamodzi ndi Iye mzakumwamba*” akutanthauza udindo wanu wovomerezeka mu Ufumu wa Mulungu. Yesu ali kudzanja lamanja la Atate, ndipo inunso ndinu thupi la Kristu. Chotero ndinu olandira cholowa pamodzi ndi Yesu mwa zonse zimene Mulungu ali nazo. Ndikudziwa kuti ndichosaneneka kuganiza za ichi, koma ndi zoonza. Muli nazo zonse; inu muli banja, ndipo ndiwo malonda abanja! Koma chifukwa mdierেকেzi wayesera kubisa zonse zomwe muliri ndi zonse zomwe muli nazo, anthu ambiri, ngakhale Akristu, amakhala ngati adamangidwabe ndi dongosolo la temberero la dziko lapansi la kupulumuka!

Fungulo imene inasintha moyo wanga inali pamene ndinazindikira kuti linali ndipo liri boma la malamulo, ndipo ine, pokhala

nzika, ndili ndi ufulu wa ulamuliro ndi phindu mu Ufumu. Malingaliro alipo abwino, ndipo ndimakonda kumva kukhalapo kwa Mulungu, koma ponena za nkhani za ulamuliro, sindifunikira kumva kuti ndapulumsidwa kuti ndipulumutsidwe. Ndi nkhani ya za ulamuliro. Sindiyenera kumva ngati ndine mmodzi wa nzika ya United States. Ndikudziwa kale kuti ndi nkhani ya ulamuliro yomwe imakwaniritsidwa ndi fundo yoti ndinabadwira kuno. Mukakhala muli bwino pamaso pa Mulungu ndipo moyo wanu wakhazikika pa lamulo mmalo mwa mmene mukumvera, zinthu zimasintha!

Ndipo uku ndi kulimbika mtima kumene tili nako kwa Mulungu: kuti ngati tipempha kanthu monga mwa chifuniro chake, atimvera. Ndipo ngati tidziwa kuti atimvera—chilichonse tichipempha—tidziwa kuti tili nazo izi tazipempha kwa Iye.

— 1 Yohane 5:14-15

Ganizirani za Lembo ili kwa mphindi; ndi limodzi mwa omwe ndimakonda. Ngati ndipempha kanthu molingana ndi chifuniro Chake, ndidziwa kuti amamva! Ichi sichikutanthauza mafunde a mawu omwe mumamva ndi makutu anu. Awa ndi mawu a ulamuliro. Taganizirani za woweruza ndi bwalo lake la milandu. Ngati woweruza wasankha kuti amvetsera mlandu, ndiye kuti wavomereza kuthetsa nkhaniyo mogwirizana ndi malamulowo. Kwa ife, popeza tapempha motsatira malamulo a Mfumu, tikudziwa kale kuti Iye adzakhazikitsa lamulo Lake. Kotero, tili ndi chidaliro pa zotsatira; sipadzakhala kungoganizira.

Mwachitsanzo, United States si ufumu chifukwa ulibe mfumu, koma umagwira ntchito motsatira malamulo omwe ali ofanana ndi

kupezeka kwa nzika iliyonse yovomerezeka. Mwanjira yofanana, Ufumu wa Mulungu umalamulidwanso ndi malamulo, omwe ali kupezeka kwa nzika iliyonse popanda tsankho. Nkhani zimene timawerenga mu Baibulo sizingotisangalatsa koma kutifotokozera malamulowo kuti tiziwaphunzira ndi kuwagwiritsa ntchito. Yesu amagwiritsa ntchito mawu akuti, “Ufumu wa Mulungu uli ngati” nthawi zambiri pamene anali kufotokozera anthu mmene Ufumuwo umagwirira ntchito. Yesu amalozera ku zamalamulo a Ufumu pamene amanena mafanizowo, ndikupereka chithunzithunzi cha mmene malamulowo anagwirira ntchito kapena kusonyeza chifukwa chimene chinachake chinachitikira. Apanso, pazifukwa zina, anthu sadziwa kuti Ufumu wa Mulungu uli ndi malamulo olamulira kagwiridwe kake ka ntchito. Anthu ambiri amaganiza kuti Mulungu akhoza kuchita chilichonse chimene akufuna pa nthawi iliyonse chifukwa iye ndi Mulungu. Ndivomereza kuti Mulungu alinazo mphamvu zochita chilichonse chimene akufuna kuchita; komabe, Iye ali ndi malire potsatira malamulo Ake. Ndikudziwa kuti izi zitha kumveka zachilendo kwa inu, koma kuti ndifotokoze fundo yanga, tiyeni tione mwachangu Maliko 6.

Yesu anati kwa iwo, “Kumudzi kwawo kokha, pakati pa abale ake ndi mnyumba mwake muli mneneri wopanda ulemu.” Sanakhoza kuchita zozizwa kumeneko, koma kuika manja ake pa odwala owerengeka ndi kuwachiritsa. Ndipo adazizwa ndi kusakhulupirira kwawo.

— Maliko 6:4-6

Pamene mukuwerenga Lembo limeneli, mumayenera kukhala

ndi zinthu zingapo zomwe zikukhudzani pokupatsani chidziwitso cha ntchito ya Ufumu.

Sanakhoza kuchita zozizwa....

Choyamba, Akristu ambiri sanaonapo Lembo limeneli ndipo angatsutsane nanu nthawi yomweyo ngati mutanena kuti ilipo nthawi ina mu Baibulo yomwe Yesu sanali kutha kuchiritsa, mungakhale kuti mukulakwitsa. Koma monga mukuonera, Iye sadakhoze. Mukamvetsetsa kuti Mfumu imagwira ntchito ndi malamulo, ndiye mumayamba kuyang'ana mozama nkhaniyi. Muyeso wakumvetsetsa kwa Akristu ambiri ndi wakuti Yesu anasankha kuti asawachiritse. Zimenezi zikadakhala zomveka ngati simukumvetsa malamulo a Ufumuwo. Kudziwa kuti Yesu anali ndi mphamvu zochiritsa koma sanatero, popanda kuzindikira mphamvu ya ulamuliro, mwachibadwe munganene kuti Iye anasankha kusachiritsa. Chinanso chingakhale chiyani?

Mwina munamvapo wina akunena kuti, “Mulungu analola kuti izi zichitike,” kapena “Mulungu ndiye amadziwa bwino kwambiri,” kapena “Zonse zili mmanja mwa Mulungu,” kapenanso mawu ena ofanana ndi awa pamene wina akunena za vuto kapena zowawa zimene iye kapena mnzake akumana nazo. Kwa Akristu wamba, apa ndi pamene amaima. Posadziwa malamulo a Ufumu ndi zimene zinalepheretsadi Yesu, fundo imodzi yokha imene ingatuluke ndiyakuti sichikadayenera kukhala chifuniro cha Mulungu kuwachiritsa. Mnzanga, Baibulo silinena kuti Iye anasankha kusachiritsa. Limanena kuti sakanatha kuwachiritsa chifukwa chosowa chikhulupiriro. Mukangozindikira kuti cholepheretsa kuchiritsa mu nkhaniyi sikusoweka kwa chifuniro cha Mulungu kuti

atero, koma mmalo mwake, panali malamulo auzimu amphamvu ya ulamuliro amene anaimitsa mphamvu ya Mulungu.

Mu nkhani zina, tsopano mudzazindikira kuti panali zifukwa zalamulo zimene mphamvu ya Mulungu inali ndi ulamuliro wobweretsa kapena kusabweretsa chifuniro Chake ndi chikhumbo chake muchochitika china, monga momwe ziliri mu ichi. Motero ndikofunika kwambiri kuti mudziwe mmene malamulo a Ufumuwa amagwirira ntchito.

Tsiku lina pamene mungadzafunire kukhudza kochokera kumwamba, simudzafuna kuti mphamvu ya kumwamba ikhale yochepa, koma kukhala ndi ufulu wotulutsa chifuniro cha Mulungu mmoyo wanu. Ndipo ndicho chifukwa chake ndinalemba bukuli.

Kuti muyambedi ulendo wanu, ndikukupangirani kuti muyambe ndi kukonza mu maganizo mwanu ndikuzindikira kuti muyenera kutaya mayankho achipembedzo akale amene mudamva mmoyo wanu wonse yokhudza chifukwa chimene Mulungu amachita

kapena sachita kanthu. Ndikukhulupirira kuti tsopano mukudziwa kuti muyenera kukana kufotokoza wamba kumene nthawi zambiri kumaperekedwa ponena chifukwa chake chimene Johnny adafa ali

**MALONJEZO AKE
AMATIPATSA LONJEZO
LA KUCHIRITSA,
KUBWEZERETSA,
KUWONJEZERKA
KWACHUMA, NDI ZINA
ZAMBIRI—OSATI
KUNGOKHALA NDI
KUTHEKERA KWA KUVUTIKA
MZOLEMETSА KAPENA
MNGOZI. CHIKONDI
CHANGWIRO CHIMAPERKA
NJIRA YOTHETSERА MAVUTO.**

wamng'ono: "Mulungu ndiye amadziwa bwino kwambiri, Iye amalamulira," ndi zina zotere. Ayi, muyenera KUDZIWA chifukwa chake chimene Yesu sakanatha kuchiritsa komanso malamulo omwe amalamulira mayendedwe a mphamvu ya Mulungu padziko lapansi. Muyenera kudziwa yankho la funso lakuti, "Chifukwa ndi chiyani Yesu sanathe kuchiritsa?" Kwa anthu ambiri, kunena kuti liripo yankho la funso limeneli kumawakhumudwitsa. Ndikungokuuzani zomwe Baibulo limanena, ndipo ndiloreni ndibwereze kuti MUYENERA kudziwa yankho la funso limenelo.

Yankho losavuta komanso lalifupi lofotokoza chifukwa chake chimene Yesu sanathe kuchiritsira mu nkhaniyo ndilakuti kumwamba kunalibe ulamuliro wochitira zimenezo. Ulamuliro umenewo umaperekedwa ndi chikhulupiriro mwa mwamuna kapena mkazi wapadziko lapansi za zimene kumwamba kukunena. Ngakhale kuti tonsefe tingavomereze kuti Yesu anali ndi mphamvu komanso anali ndi chikhumbo chochiritsa anthu, Iye sakanatha. Yesu, Mwini ananena kuti kulephera kuchiritsa sikunali chifooko ku mbali Yake koma chinali chifukwa chakuti anthu analibe chikhulupiriro. Lembani zimenezo! Pali fungulo yaikulu pamenepa! Chikhulupiriro!

Mu buku langa lakumbuyo, ndinatenga nthawi yaikulu kufotokoza kuti chikhulupiriro ndi chiyani, mmene chimagwirira ntchito, chifukwa chake timafunira chikhulupiriro, chifukwa chake chimene Mulungu amafuna chikhulupiriro, mmene timapezera chikhulupiriro, ndi mmene timadziwira ngati tili mu chikhulupiriro. Kunena kuti kumvetsetsa kwanu lamulo lofunika kwambiri la Ufumu umenewu, kungakhale kuchepsa fundoyi. Ndi moyo ndi imfa!

Posachedwapa ndinalandira kalata ya nkhani zochokera ku utumiki waChikristu wodziwika bwino. Mwatsoka, zimene zinali

mkati mwake zinali zofanana ndi zomwe Akristu ambiri amakhulupirira. Ndiloreni ndigawane nanu zina pano.

Imayamba ndi mawu akulu ochokera pa **Deuteronomo 31:6**:

Khalani amphamvu ndi olimba mtima. Musamachite mantha kapena kuopsedwa chifukwa cha iwowa, popeza Yehova Mulungu wanu ndiye amene amuka nanu. Iye sadzakusowani kapena kukusiyani.

Kenako imapitilira kunena kuti...

“Ndi chifukwa chiyani Mulungu saletsa uchigawenga ndi kuvutika? Ndi chifukwa chiyani amalola kuti anthu azifa? Mafunso ndi ochuluka, ndipo choonadi chake ndichakuti sitikudziwa mayankho ake onse. Sitikudziwa chifukwa chake Mulungu amalola kuti zinthu zina zichitike. Chimene tikudziwa ndichakuti chikondi cha Mulungu ndi changwiro. Njira zake zili pamwamba pa njira zathu. Tiyenera kudalira malonjezo ake amene amatiuza kuti sadzati-patsa zoposa zimene tingathe kukhala nazo, koma kuti chilichonse chimene watipatsa, chidzakhala nafe nthawi iliyonse.”

ZOLAKWIKWA, ZOLAKWIKWA, ZOLAKWIKWA! Ndipotu Baibulo limatiuza zosiyansiratu ndi zimenezi.

Sichinakugwerani inu chiyeso koma cha umunthu; koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza; koma ndi kuyesedwa adzakonza njira yopulumukira, imene mudzatha kuipirira.

— 1 Akorinto 10:13 (NKJV)

Malonjezo Ake amatipatsa lonjezo la kuchiritisa, kubwezeretsa, kuwonjezereka kwachuma, ndi zina zambiri—osati kungokhala ndi

kuthekera kwa kuvutika mzolemetisa kapena mngozi. Chikondi changwiro chimapereka njira yothetsera mavuto. Ndikhoza kupitiriza, koma izi, mwatsoka, ndi zomwe anthu ambiri amakhulupirira za Mulungu. Kodi munthu angaganize bwanji kuti Mulungu, yemwe chikondi chake ndi changwiro, angapatse munthu khansa kapena kukana kuchiritsa pamene ali ndi mphamvu zochitira zimenezo, ndizosatheka. Atafunsidwa za izi, yankho lawo lanthawi zonse ndilakuti njira Zake siziri njira zathu. Mukuseleura? Tilibe chikondi changwiro ndipo sitingachite zimenezo kwa mwana wathu! Mmalomwake, amapanga njira Zake momveka bwino m'Mawu Ake.

Kalata yankhaniyo inatanthauza kuti chilichonse chimene angatipatse, iye adzakhalapo nthawi zonse pamene tikuvutika. Kodi Mulungu adzatipatsa chinthu choipa? Ayi. Baibulo limatiuza kuti iye ali nafe ndipo sadzatisiya, zitanthauza kuti Mulungu ali nafe kutsimikizira malonjezo Ake! Mnzanga, chiphunzitso chakuti Mulungu ndi mdani wathu sichichokera kwa Mulungu. Sichi-maimira Mulungu amene ndimamutumikira, ndipo ndikukhulupirira kuti simudzapirira nacho. Ngati mpingo wanu umaphunzitsa zosayenera zotere, muyenera kuchokamo nthawi yomweyo!

Mulungu ndiye chikondi ndipo Mawu amanena kuti chikondi sichilephera. Komabe, chimene chimalephera, ndi ulamuliro wa Mulungu, mphamvu Yake yolowererapo padziko lapansi, imene imapangidwa ndi chikhulupiriro chathu. Apanso, iyi ndi nkhani ya za ulamuliro, osati nkhani yoopsa, nkhani yakumva, kapena china chilichonse. Ndi nkhani ya ulamuliro chabe imene muyenera kuidziwa. Popeza munthu ali ndi ulamuliro padziko lapansi, Mulungu sangangochita zimene akufuna, monga ndagawana nanu. Mgwirizano wanu ndi Kumwamba, chikhulupiriro chanu, ndichofunika kuti chipereke mphamvu zakumwamba kuti zibweretse

mphamvu ya Mulungu mchochitikacho ndikubala chilungamo. Mnzanga, **uyenera** kudziwa kuti chikhulupiriro ndichiyani komanso ndi chifukwa chiyani chili chofunikira polandira kuchokera kwa Mulungu.

Mwina simunawerenge buku langa lakumbuyoku (*Kusinthika kwa chuma Chanu: Mphamvu ya Kukhulupirika*), ndiloreni ndibwerezenso mwachidule za chikhulupiriro. Ngakhale mungaganize kuti pafupifupi Mkristu aliyense wogwiritsa ntchito liwu loti *chikhulupiriro* angadziwe kuti ndi chotani, mukhoza kukhala olakwa. Tifunika kukhala ndi phunziro la mbiri yake kuti tithe kumvetsetsa fundo yofunika kwambiri ya Ufumu pa nkhani ya mphamvu ya ulamuliro.

Tiyeni tione **Aroma 4:18-21:**

Popanda chiyembekezo chilichonse, Abrahamu anakhulupirira mwachiyembekezo ndipo anakhala Tate wa mitundu yambiri ya anthu, monga kunanenedwa kwa iye kuti, “Chomwecho mbewu yako idzakhala yotere.” Popanda kufooka mu chikhulupiriro chake, iye anaona chenicheni chakuti thupi lake linali ngati lakufa—popeza anali ndi zaka pafupifupi zana limodzi—ndiponso kuti mimba ya Sara inali youma. Koma sanagwedezeke chifukwa cha kusakhulupirira kwa lonjezo la Mulungu, koma analimbikitsidwa mu chikhulupiriro, nalemekeza Mulungu, nakhazikikanso mmtima kuti Mulungu adali nayo mphamvu yakuchita chimene adalonjeza.

Abrahamu amadziwika ngati tate wa chikhulupiriro chathu. Iye anali wokhazikika mumtima kuti Mulungu adali nayo mphamvu yakuchita chimene adalonjeza. Kukhala wokhazikika mumtima, mogwirizana ndi Mulungu, kumatchedwa chikhulupiriro. Popanda

mgwirizano umenewo, Mulungu sangangomayenda m'dziko lapansi. Ndiye mungafunse kuti, “Ndi chifukwa chiyani Mulungu angafune kuti wina aliyense achite chilichonse chimene chingamulore kuti achite chinachake kapena kumulepheretsa kuchita chilichonse chimene wasankha? Iye ndi Mulungu.” Kutu tiyankhe funso limeneli, tifunika kuyang'ana mwamsanga kumbuyo pachiyambi, mu nthawi ya Adamu.

Mudamchepa pang'ono ndi angelo, munamveka iye korona wa ulamuliriro ndi ulemu, ndipo mudamuika iye woyang'anira ntchito za manja anu. Mudagonjetsa zonse pansu pa mapazi ake. Pakuti muja adagonjetsa zonse kwa iye, sanasiyapo kanthu kosamgonjera iye. Koma sitinayambe tsopano apa kuona zonse zimgonjera.

— Aheberi 2:7-8

Lembo limeneli likunena za Adamu ndi Hava pachilengedwe. Chonde dziwani kuti panalibe chilichonse padziko lapansi chomwe sichinali pansu pa ulamuliro wawo. Adamu anaikidwa padziko lapansi kuti alamulire dziko lapansi ndi ulamuliro wopatidwa mmalo mwa Ufumu wa Mulungu. Iye analamulira dziko lonse lapansi.

Ndipo anati Mulungu, “Tipange munthu mchifanizo chathu, monga mwa chikhalidwe chathu, alamulire pansomba za m'nyanja, ndi pambalame za m'mlengalenga, ndi pang'ombe, ndi padziko lonse lapansi, ndi pazokwawa zonse zakukwawa padziko lapansi.”

— Genesis 1:26

Apanso, tikuona kuti Adamu analamulira dziko lapansi ndi ulamuliro wopatsidwa ndipo anavekedwa korona wa ulemerero (kudzozedwa kapena mphamvu) ndi ulemu (udindo wa ulamuliro). Panalibe chilichonse chimene sichinali pansu pa ulamuliro wake. Ndipotu, mukamawerenga nkhani ya chilengedwe, Adamu anapatsadi maina nyama monga anali padziko lonse lapansi. Monga tonse tikudziwira, Adamu anataya ulamuliro wake chifukwa cha Satana, amene ananyenga Hava ndi kuyesa Adamu kuukira boma la Mulungu, chimene iye anachita. Paulo akulemba mu 2 Akorinto 4:4 kuti Satana, kupyolera mkuukira kwa Adamu, anakhala mulungu wa dziko lapansi. Iye sananene kuti iye anali mulungu, koma mmalo mwake, mulungu wa dziko lapansi, kutanthauza kuti anali ndi ulamuliro wa uzimu wovomerezeka pano. Ngakhale kuti munthu adakali ndi moyo padziko lapansi, mwauzimu, anali wakufa kwa Mulungu. Mzimu wa munthu, umene unalengedwa kuyenda mu umodzi ndi Mzimu wa Mulungu, tsopano unapatulidwa kwa Iye. Munthu anayamba kuyenda monga momwe amamverera, malingaliro ake, nzeru zake, chifuniro, ndi machitidwe.

Ndipo mmene anamtsogolera anakwera naye namuonetsera Iye maufumu onse a dziko lokhalamo anthu mkamphindi kakang'ono. Ndipo mdierekezi anati kwa Iye, "Ine ndidzapatsa Inu ulamuliro wonse umenewu ndi ulamuliro wawo: chifukwa unaperekedwa kwa ine; ndipo ndiupatsa kwa iye amene ndifuna. Chifukwa chake ngati inu mudzagwadira pamaso panga, wonsewo udzakhala wanu."

— Luka 4:5-7

Mudzaona kuti Satana akunena kuti udindo umene ali nawo

pa dziko lapansi “**unaperekedwa**” kwa iye. Ndithudi, tikudziwa kuti amene anamupatsa anali amene mwalamulo anali nawo pachiyambi, ndipo anali Adamu. Ichi ndichofunikira. Ndipotu, ngati, Satana akanafuna kuti alowe mdziko lapansi mosaloledwa, akanaponyedwa kunja nthawi yomweyo ndiponso mokankhidwa. Ngati mungaganizire wapolisi akuitanira womthandizira, mudzakhala ndi lingaliro labwino la chifukwa chomwe ndikunena kuti Satana anakankhidwira kunja. *Badge* yomwe mkuluyo amavala imatanthauza kuti asilikali onse ndi mphamvu za boma la United States zilipo kutsimikizira mawu ake.

Korona amene Adamu anavala (udindo umene anali nawo), kulamulira mmalo mwa boma la Mulungu, anabweretsa mphamvu zonse za Mulungu kuti zimuchirikize. Chifukwa cha udindo wa Adamu padziko lapansi, Satana analibe ulamuliro uliwonse padziko lapansi. Analamulidwa ndi Adamu ndi Hava. Njira yokhayo yovemerezeka ya Satana yopezera ulamuliro mdziko lapansi ikafunikira kuti Adamu avule korona yachifumu wake, imene Satana analibe ulamuliro wakumkakamiza kuchita. Satana anadziwa kuti munthu yekhayo amene akadachotsa koronayo pa mutu wa Adamu anali Adamu mwini. Ndicho chifukwa chake Satana anayenera kugwiritsa ntchito njira yake yachinyengo. Kodi chinyengo chime-necho chinali chiyani? Satana anali kutanthauza kuti Mulungu ndi wosadalirika komanso kuti sanali kuwafunira zabwino. Iye anakhutitsa Hava kuti panali phindu pa kusamvera Mulungu ndi kuti malamulo a Mulungu anali kulepheretsa iye ndi Adamu kuchita kanthu kena kopindulitsa.

Satana anachititsa Adamu ndi Hava kukhulupirira kapena kugwirizana ndi iye mmalo mwa Mulungu.

Mosavuta, ichi ndi chikhulupiriro. Chikhulupiriro chingatanthauzidwe kukhala “kukhazikika mumtima” za zimene Mulungu amanena. Adamu ndi Hava anasiya Mawu a Mulungu monga odalirika ndipo mmalo mwake anayamba kugwirizana ndi zimene Satana ananena. Kenako adachita zomwe adakhulupirira, zimene zidawachotsera ubwino wawo mu Ufumu wa Mulungu ndi kumpatsa Satana malo pa zochita za anthu. Chotsatira? Adamu, amene anali ndi ulamuliro pa dziko lapansi, anachotsa Mulungu mwauzimu pamene anagwirizana ndi Satana! Adamu anasiya korona wake, malo ake a ulamuliro, natsatira Satana. Mwakutero, iye anachotsa Mulungu mu moyo wake. Anthu ambiri anganene kuti, “Ayi, sizikadachitika; Adamu sakadatha kuchotsa Mulungu padziko lapansi!” Koma ponena za zochita za anthu, adachitadi zimenezo. Ndiloreni nditsimikizire ichi kwa inu. Tiyeni tionenso **Genesis 3:17-19**. Adamu atachimwa, Mulungu anapita kwa iye nati,

Nthaka ikhale yotembereredwa chifukwa cha iwe; chifukwa cha zowawa udzadyako masiku onse a moyo wako. Idzakuberekera minga ndi mitula, ndipo udzadya zomera zakutchire. Mu thukuta la nkhope yako udzadya chakudya, kufikira udzabwerera kunthaka, popeza kuti unatengedwa; pakuti ndiwe fumbi, ndi kufumbiko udzabwerera.

Taonani akuti, “*Nthaka [dziko lapansi] ikhale yotembereredwa chifukwa cha iwe.*”

Kutembereredwa kumangotanthauza kusakhalapo kwa nkhope ya Mulungu ndi madalitso. Ndi Adamu, amene anali ndi ulamuliro

pa dziko lapansi, amene anadula ulamuliro wovomerezeka wa Mulungu pa dziko lapansi. Kwenikweni, Mulungu akuti, “E-ee, Adamu, chifukwa cha iwe, manja anga ali omangidwa. Sindingathe kukuthandiza.” Kenako akuuza Adamu kuti kupulumuka kwako kudzakhalala kwa iyeyo, akuchita ntchito yolemetsa ndi yowawa. Izi ndikuziticha “dongosolo la temberero lapadziko lapansi” yopulumukira. Apa ndi pamene tonse tinakulira—mu ufumu wa kupulumuka ndi mantha. Tinaphunzira kuda nkhawa, ndipo mantha akhala akulamulira maganizo athu kuyambira pamene tinabadwa. Ndikufuna kuti ndibwererenso ku Lembo ili pang’ono kuti tikambirane za dongosolo la temberero la dziko lapansi, koma pakadali pano, ndikufuna ndikutsimikizireni kuti mumvetsetse momwe Satana adalowera padziko lapansi. Apanso, anafunikira kupeza mwamuna kapena mkazi padziko lapansi amene anali ndi mphamvu ya ulamuliro wopatsidwa ndi Mulungu mdziko lapansi kumtsegulira khomo. Adamu anali ndi fungulo imeneyo, ndipo Satana anakwanitsa kunyenga Adamu kuti atsegule chitsekochi. Tsopano, tiyeni tionenso Aheberi 2:7-8.

Mudamchepesa pang’ono ndi angelo, munamveka iye korona wa ulamuliriro ndi ulemu, ndipo mudamuika iye woyang’anira ntchito za manja anu. Mudagonjetsa zonse panso pa mapazi ake. Pakuti muja adagonjetsa zonse kwa iye, sanasiyapo kanthu kosamgonjera iye. Koma sitinayambe tsopano apa kuona zonse zimgonjera.

— Aheberi 2:7-8

Zindikirani kuti Lembo ili likunena kuti Sanasiyapo kanthu

kosamgonjera iye. Ngakhale kuti Lembo limeneli likunena za chochitika kale, limagwiritsa ntchito liwu loti *liri* mu nthawi yamakono kufotokoza mmene munthu aliri padziko lapansi pano. Ngakhale kuti munthu anataya ulamuliro wake wauzimu mdziko lapansi chifukwa cha uchimo wa Adamu, munthu sanataye kukhala kwake kwa ulamuliro ya dziko lapansi lenilenilo, motero kugwiritsidwa ntchito kwa liwu *liri*. Chifukwa cha kaimidwe kalamulo kameneka kamene munthu ali nako pa dziko lapansi, ndi chifukwa cha ulamuliro wa uzimu wa Satana pa anthu, Mulungu sangangobwera mwadzidzidzi mdziko lapansi ndi kuphwanya Mawu Ake kapena kuti Satana angadzinene kuti sanachite bwino.

Mulungu ayenera kupeza mwamuna kapena mkazi mdziko lapansi amene adzagwirizana Naye, zimene zimatsegula khomo la uzimu kuti Ufumu wa Mulungu ukhale ndi ulamuliro pano. Monga momwe Satana anafunikira kugwira ntchito kupyolera mwa mlonda wa pachipata, Adamu, Mulungu tsopano ayenera kugwira ntchito kupyolera mwa amuna ndi akazi, alonda a zipata za dziko lapansi, kuti apereke ulamuliro wa Ufumu pano. Kukhala ndi mtima ndi malingaliro anu okhazikikanso ndi zomwe kumwamba kunena chimatchedwa chikhulupiriro. Chikhulupiriro chiyenera kukhalapo kuti Ufumu wa Mulungu ukhale ndi mphamvu ya ulamuliro pano. Sinditenga nthawi pano kuti ndifotokoze momwe mungapezere chikhulupiriro kapena momwe mungadziwire ngati muli mu chikhulupiriro. Zonsezi zafotokozedwa mu buku langa loyamba la mndandanda wa mabuku ano. Pacholinga cha kukambiranaku, ndikungofuna kutsimikizira kuti mukudziwa kuti chikhulupiriro ndi chiani komanso chifukwa chake chimene chili chofunikira kuti kumwamba kusamukire pano padziko lapansi.

Tsopano, ndikuyembekeza kuti mukumvetsa bwino chifukwa chake Yesu “sanathe” kuchita zozizwitsa zambiri kumudzi kwawo—anthu kumeneko analibe chikhulupiriro. Chotero kumwamba kunalibe mphamvu ya ulamuliro. Ndiloreni ine nditsirize zokambiranazi ndi Lembo lalikulu lomwe lionetsere zomwe ndikunena.

Aliyense wamva za Aroma 10:10:

Pakuti ndi mtima munthu akhulupirira kutengapo chilungamo, ndi m’kamwa avomereza kutengapo chipulumutso.

Lembo limeneli ndi mbali ya njira imene Akristu amatcha msewu wa Aroma, ndipo ndi mbali ya Malembo anayi amene amatisonyeza mmene tingapulumukire. Koma kodi mwaimadi ndi kulingalira za njira imene Aroma 10:10 akusonyeza? Ndi mtima wanu ummene mumakhulupirira kapena kulowa mu mgwirizano ndi kumwamba. Mtima wanu pogwirizana ndi kumwamba kumapangitsa kukhala kovomerezeka kuti kumwamba kulowe padziko lapansi. Lembo ili likuti ukakhulupirira kumwamba, umakhala wolungama. Chilungamo ndi kayendetsedwe ka lamulo. Choncho kukhulupirira mu mtima mwanu kumakupatsani ufulu wa ulamuliro pamaso pa kumwamba ndi dziko lapansi kuti mukhale ndi zomwe kumwamba kukunena chifukwa kumapereka chilolezo chakumwamba padziko lapansi. Koma zindikirani palibe chomwe chingachitikebe. Pali gawo lachiwiri ku Lembo limeneli: “...*ndi m’kamwa avomereza kutengapo chipulumutso.*” Mukuona, ngakhale kuti mtima wanu ukhoza kugwirizana ndi kumwamba, kumene kumapangitsa kukhala kovomerezeka kuti kumwamba kulowe pa dziko lapansi, palibe chimene chimachitika mpaka inu, mwamuna kapena mkazi mdziko lapansi amene ali ndi ulamuliro pa dziko lapansi, atatulutsa

zimenezo mdziko lapansi. Chifukwa chiyani? Chifukwa muli nawo ulamuliro pano; kumwamba sikungachite popanda inu!

Indetu, ndinena kwa inu, Zilizonse mukazimanga padziko lapansi zidzakhala zomangidwa Kumwamba; ndipo zilizonse mukazimasula pa dziko lapansi zidzakhala zomasulidwa kumwamba.

— Mateyu 18:18

Kwenikweni, uku ndi kunena kumene ndangokamba. Chilichonse mumanga padziko lapansi, kumwamba kudzachikhazikitsa, ndipo chilichonse mumasula padziko lapansi, kumwamba kudzachikhazikitsanso. Kumwamba sikungachite popanda inu. Kumwamba kuli kukuyembekezerani ndipo sikungasunthe pokhapokha mwamuna kapena mkazi amene ali mchikhulupiriro kapena m'ngwirizano ndi kumwamba atulutsa ulamuliro umenewo ku dziko lapansi.

Kumvetsetsa momwe ulamuliro ndi mphamvu zakumwamba zingatulutsidwe kudziko lapansi kumapangitsa kusiyana konse. Zinachita mmoyo wanga ndipo zidatero mu *email* yotsatira yomwe ndidalandira.

“Moni! Mwamuna wanga ndi ine tikufuna kugawana nanu nkhani yathu yodabwitsa ya 'chikhulupiriro chakusaka'! Mu 2011, tinali kukhala 'mnyumba yathu yamaloto,' koma tinali kukhala ndi ndarama zochepa ndipo nthawi zina tinali kugwiritsa ntchito makhadi angongole pogulira zinthu komanso [kutenthetsa] nyumba yathu. Tinali kungokhalabe choncho koma osatukuka. Ndinali mtsogoleri wachipembedzo mtchalitchi chathu, koma chikhulupiriro chathu sichinali chogwirizana ndi ndarama zathu. Ndinaona *programme* yanu *Fixing the Money Thing* pa Daystar,

yomwe idandigwira mtima, ndipo [ndina]itanitsa bukulo, *Fixing the Money Thing*, pamodzi ndi ma CD a *Kusinthika kwa Chuma*. Nthawi zonse tinali kumvetsera ma CD amenewa pamene timaw-
rengerana bukulo.

“Sitinadziwe kuti sitinali mu chikhulupiriro! Tinadziwa kuti tisunge nyumba ya maloto imeneyi, tinafunikira mayankho a mmene ndarama zimagwirira ntchito mu Ufumu. Tinafesa mbewu ya \$200 mu Faith Life Ministries (yomwe ingakhalenso [yakhala] \$2,000. Izo zinali ndarama zambiri kwa ife mnthawi imeneyo! Ndipo mgwirizano ndi Mulungu unali wakuti ationetse malonda ochitira kunyumba.

“Mulungu anatipatsa lingaliro la malonda lolera ana agalu a *Goldendoodle* kunyumba kwathu. Tinagula ana agalu 2 a *Goldendoodle*, Bella ndi Gracie, kuwalera kuti abereke ana agalu a *Goldendoodle*, ndipo tinagwirizana ndi Mulungu. Tidadziwa kuti sitingapange tiana!! Tinaweta ma *doodle* athu awiri, ndipo mu 2014, tinali ndi ana 13 oti tigulitse pamtengo wamsika \$1,200 mmodzi. Chaka chino, 2015, takhala ndi ana agalu 63, ONSE athanzi. Kuchokera kukugulitsa ana agaluwa, tamasuka ku ngongole zathu zonse kupatula ya nyumba yathu. Tsopano tinalinso ndi thumba la ndarama ladzidzidzi.

“Tinadabwa kuti mayi anga anatifunsa ngati tingafune kuti mtundu wawo wa *Goldendoodle* ubereke chifukwa anali kupuma pantchito! Mulungu adatidalitsa ndi ena 2 *doodles* aulere! Ndipo mu July, mwamuna wanga adakwezedwa kukhala woyang’anira ku sukulu yathu!! Mchaka chimodzi, ndarama zomwe timapeza zidakwera mowirikiza kufika pa number zokwana 6!! KUSAKA NDI CHIKHULUPIRIRO KUMAGWIRA NTCHITO!! Tinalowa mmalamulo a Ufumu wa Mulungu. Tsopano, timafesa mu mitundu yonse ya ntchito za Ufumu ndi kupezeka ku tchalitchi chanu pa

internet Lamlungu lililonse mmawa tisanatsogolere chipembedzo mu tchalitchi chathu! Zikomo kwambiri chifukwa chotiphunzitsa mmene Ufumu umayendera!”

—Karla

Banja lomweli landitumizira *email* yotsatira sabata ino.

“Pasaka yabwino! Wauka! Tinali kufuna kugawana zochitika za Mbusa wathu Gary pa *internet*! Chonde mudziwitseni kuti tinakondwerera kubadwa kwa Yesu ku Yerusalemu chaka chino (zonse zinalipiridwa). Tinadalitsidwanso mwana wathu wachinyamata Carter pobatizidwa mu Mtsinje wa Yordano, ndi kupembedza pamodzi ndi Hillsong Australia pa Nyanja ya Galileya madzulo! O-oo!!! Ndikuthokoza kwambiri kuti tinakonza zinthu za ndarama!

Takhala ndi ana agalu zana ndi makumi awiri mphambu imodzi tsopano. Tinayenera kukweza mtengo wa mwana wagalu kufika pa \$2,300 chifukwa mndandanda wa ofuna agalu unali wautali kwambiri! Tamandani Mulungu.”

—Karla

Ichi ndi chitsanzo chabwino kwambiri cha zimene Ufumu udzachite pa moyo wanu. Ndinaimbira Karla foni sabata lino nditalandira *email* iyi, ndipo iye anali wokondwa KWAMBIRI!!! Anati nyumba yawo ilipiridwa chaka chino. Mukayang’ana *email* yoyamba yomwe adatumiza, adanena panthawiyo zotsatirazi (zotchulidwa pa *email* yomwe ili pamwambayi):

“Tinali kukhala ndi ndarama zochepa ndipo nthawi zina tinali kugwiritsa ntchito makhadi angongole pogulira zinthu komanso [kutenthetsa] nyumba yathu. Tinali kungokhalabe choncho koma osatukuka.”

Tsopano, patangopita zaka zingapo, adzakhala atailipira? Ufumu!

MUTU 3

UFUMU NDIWO YANKHO LANU

Tsopano popeza mwamvetsetsa bwino momwe Ufumu umagwirira ntchito ndi malamulo komanso fundo zomwe sizisinthana, ndikufuna kuti ndiyambe kuyang'ana pa malamulo omwe amakhudza kwambiri ndarama zanu, ndipo, pamapeto pake, mpumulo wanu.

Koma tisanapite kumeneko, ndikufuna kufotokoza chifukwa chake ndinatcha bukuli *Mphamvu ya Mpumulo* ndi zomwe ndikutanthauza ndi mawu akuti *mpumulo* pa nkhani ya zachuma ndi Ufumu. Chodabwitsa ndi chakuti, siine amene ndinayambitsa lingaliro limeneli pankhani ya zachuma, Mulungu anatero.

Ndipo zinatha kupangidwa zakumwamba ndi dziko lapansi ndi khamu lawo lonse. Tsiku lachisanu ndi chiwiri Mulungu anamaliza ntchito yonse anaipanga; ndipo anapuma

tsiku lachisanu ndi chiwiri ku ntchito yake yonse. Mulungu ndipo anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri, naliyeretsa limenelo, chifukwa limenelo anapuma ku ntchito yake yonse imene Mulungu anailenga ndi kupanga.

— Genesis 2:1-3

Choyamba, ndiloreni ndifotokoze momveka bwino kuti: Mulungu sanapume pa tsiku lachisanu ndi chiwiri chifukwa chakuti anali wotopa. Mulungu saatopa. Anapumula chifukwa, monga liwuli likunenera, chilichonse chinali chitatha ndipo Iye anatsiriziratu. Analenga munthu kumapeto kwa tsiku lachisanu ndi chimodzi la chilengedwe kuti akhale ndi moyo pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Tsiku lachisanu ndi chiwiri linalibe lingaliro la mantha, kuganiza za moyo, matenda, ndi ntchito yowawa kapena kukhetsa thukuta kuti tipeze zofunikira. Mmalowake, maganizo a Adamu akadangkhalala pa Mulungu, mkazi wake, ntchito yake, ndi cholinga. Chilichonse chimene anafuna kuti chilimbikitse ntchito yake ndi moyo wake zinakonzedwa ndipo zinalipo; dongosolo la Mulungu linali lathunthu. Masiku ano anthu amalota kukhala ndi zomwe Adamu anali nazo, moyo wopanda nkhwawa ya chisamaliro, kukhala ndi luso loyang'ana pa zowakhudza zawo ndi maubale popanda chidandaulo pa zofunikira. Mwa tsoka, pamene Adamu anapanduka, anataya zofunikira za Mulungu, ndipo munthu wakhala akukakamizika kuthamangathamanga (ntchito zowawa ndi kukhetsa thukuta) kufunafuna zinthu zopezetsa moyo kuyambira pameneipo.

Pakuti anthu akunja azifunitsa zonse zimenezo, pakuti Atate wanu wa Kumwamba adziwa kuti musowa zonse

zimenezo. Koma muthange mwafuna Ufumu wake ndi chilungamo chake, ndipo zonse zimenezo zidzawonjezedwa kwa inu.

— Mateyu 6:32-33

Kuvuta kwakupeza zofunikira ndi katundu wolemetsa ndipo kumasokoneza malingaliro a moyo a munthu. Chokopa cha chuma, kukhala omasuka ku ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta pa zofunika pa zopulumukira, ndizo zimene anthu amalota. Kukhala *millionaire* kokha kuli ndi tanthauzo ndi kuthekera kwake kochepetsera kupsinjika ndi vuto lopezera zofunikira, kumatilola kuyang'ana pa cholinga ndi ntchito. *Lottery* ndiyotchuka kwambiri chifukwa imapereka mwayi wokhala nazo zinthu opanda kuchita ntchito komanso kukuthawitsa ku dongosolo la temberero la dziko lapansi la zachuma. Ndongomeko za kulemera-mwachangu ndi zochuluka mwa mtundu uli wonse ndipo nthawi zonse zimadzadza ku ma *email* athu ndi zolemba za *Facebook*. Chotero mu nkhani ya ndarama zathu, tiyenera kuyankha funso lakuti: Kodi ilipo njira yobwerera ku tsiku lachisanu ndi chiwiri limene chilichonse chili chokwanira ndi chokhazikika ndi chopezeka? Yankho ndi INDE Wamkulu! Mmene zimenezo zimachitikira ndi kumvetsetsa malamulo a Ufumu amene adzabweretse zipatso, ndicho cholinga cha bukuli. Ndikudziwa zomwe mwakumana nazo mmoyo kapena mmpingo komanso Akristu angatsutse kuti zomwe ndikunena

**MAYANKHO ONSE
OMWE MUNGAFUNE
KUTI MUCHITE BWINO
NDI KUCHITA BWINO PA
NTCHITOYI, KUKULOLANI
KUTI MUZINDIKIRE
CHOLINGA CHANU, ALI
MU UFUMU.**

sizingakhale zoon, monga momwe Akristu ambiri adavomereza chiphunzitso chaumulungu kuti “umphawi ndi woyera.” Koma ndikukutsimikizirani kuti mayankho onse omwe mungafune kuti muchite bwino ndi kuchita bwino pa ntchitoyi, kukulolani kuti muzindikire cholinga chanu, ali mu Ufumu.

Odala osauka inu, chifukwa uli wanu ufumu wa Mulungu.
— Luka 6:20

Yankho la kusauka ndiwo Ufumu! Ili ndi Lembo loyamba limene Mulungu ananditsogolera pamene anayamba kundiphunzitsa lamulo la zachuma la Ufumu. Inde, kuti mumvetse lingaliro ili, muyenera kudziwa tanthauzo la lingaliro la ufumu, lomwe ndatchula kale. Ndipo ndikuganiza muli ndi kumvetsetsa kwabwino pa zomwe zidachitika kwenikweni ku Munda pamene Adamu adachimwa. Tsono ndiloreni mwakamphindi kuti ndiunikenso mwachangu.

Pachiyambi, Adamu ndi Hava sanali kudera nkhawa chilichonse; panalibe matenda ndipo panalibe zofunikira kuti zidye malingaliro awo tsiku lililonse. Tsiku lililonse anali kungofunika kuganizira ntchito yawo, imene inali kukonda Mulungu, kukondana, ndi kusamalira dziko lapansi ndi Munda umene Mulungu anawapatsa. Mantha munalibe mmiyoyo yawo. Koma pamene Adamu anachita chiwembu, zonse zinasintha ndithu. Monga ndidanenera, satana adakhala mulungu wadziko lino, munthu adachotsedwa kwa Mulungu, ndipo Mulungu adachotsedwa pakukhala ndi mphamvu ya ulamuliro pa munthu. Adamu anadabwa mu chenicheni cha chatsopano cha momwe moyo umagwirira ntchito. Apanso, awa ndiwo mawu amene Mulungu anabweretsa kwa Adamu atachimwa.

Nthaka ikhale yotembereredwa chifukwa cha iwe; chifukwa cha zowawa udzadyako masiku onse a moyo wako. Idzakuberekera minga ndi mitula, ndipo udzadya zomera zakutchire. Mu thukuta la nkhope yako udzadya chakudya, kufikira udzabwerera kunthaka, popeza kuti unatengedwa; pakuti ndiwe fumbi, ndi kufumbiko udzabwerera.

— Genesis 3:17-19

Kugwira ntchito yowawa, kukhetsa thukuta, mantha, nkhwawa, ndi malingaliro a akupuluka ndi zomwe zimadya malingaliro a Adamu ndi Hava. Cholinga chawo, chomwe chinali chikonzero cha Mulungu kwa iwo, tsopano chidataika pa mpikisano ndi nkondo yakupulumuka. Kufuna chisamaliro ndikupeza zofunikira, zinalowa mmalo a ntchito yodabwitsa ya Adamu komanso cholinga chake. Adataya kudzionka kuti ndi ndani. Cholinga chokhacho chomwe adachiona tsopano ndicho kukhala ndi moyo, chomwe chidafunikira kugwira ntchito zowawa komanso zokhetsa thukuta nthawi zonse. Palibe zambiri zomwe zasintha kuyambira tsiku limenelo mpaka pano.

Masiku ano, monga mbusa, ndimaona kuti funso lalikulu limene anthu amandifunsa ndi lakuti, “Kodi ndiyenera kuchita chiyani pa moyo wanga?” Chifukwa chomwe amafunsira ndi chifukwa chakuti padziko lapansi chiyambire Adamu, kufunafuna zofunikira ndicho cholinga cha chomwe chilichonse chimayesedwera. Zitsimikizo zimapangidwa pazifukwa za ndarama osati zolinga. Ndarama ndi kufunika kwake zingakakamize anthu kugwira ntchito zomwe amadana nazo. Kunena zoona, anthu ambiri alibe chithunzithunzi kwenikweni kuti iwo ndi ndani. Lembani izi, “Mpaka inu mutamudziwa Mulungu, simudzadziwa konse mapangidwe Ake pa moyo wanu. Iye ndi amene adakulengani.”

Anthu ali ndi njala yaikulu yofuna kudziwa kuti iwo ndi ndani. Padziko lapansi amaoneka ngati owerengeka chabe, koma kwa Mulungu iwo ndi okonedwa kwambiri ndipo ndiwo chilengedwe chapadera chokhala ndi luso komanso kuthekera komwe palibe wina aliyense ali nako. Koma chifukwa chakuti sadziwa Mulungu ndipo, motero, sazidziwa iwo eni, amayang'ana kufunika kwawo mmalo onse olakwika. Amalola chikhalidwe kulamulira kufunika kwawo povomereza zomwe chikhalidwe chimanena. Koma chithunzi chomwe atolankhani amaonetsa ndi kalilole wachikhalidwe zonsezo ndi mithunzi yosunthika. Pamene mukuganiza kuti mukuyenda mogwirizana ndi zomwe zimati ndi zovomerezeka, mudzapeza kuti zasintha ndipo inu muli kumbuyo.

Ndikukumbukira ndili ku Paris ndikuyenda mumsewu ndi Drenda. Paris, ndithudi, umadziwika ndi fashoni; ndipo mafashoni a chaka chimenecho anali otuwa ndi akuda. Zenera lililonse lasitolo linali lodzaza ndi zotuwa ndi zakuda zokha. Pamene ndinayang'ana mumsewu, mbali zonse ziwiri, ndinatha kuona mazana a anthu akuyenda. Ndinadabwa kuona kuti palibe ngakhale kansalu kakang'ono ka mtundu wina. Munthu aliyense anali atavala zotuwa ndi zakuda. Panali mazana ndi mazana a anthu omwe anali kuoneka mofanana. Kodi ndi liti pamene wina anakuuzani kuti mtundu wake womwe amaukonda ndi wotuwa? Koma tsiku limenelo, anthu ambiri anali otsimikiza kuti zomwe amakonda zinali zotuwa kapena zakuda.

Chifukwa chakuti chipanikizo cha kupeza zofunikira ndi champhamvu kwambiri ndipo chimasokoneza umunthu wathu ku chilichonse chimene tikuganiza kuti chingatithandize kuchipeza ndi kulandiridwa, ine ndi Drenda tinapanga mwambi umene takhala tikulalikira kwa zaka zambiri: “ngati simukonza za ndarama,

simudzazindikira tsogolo lanu!” Kukhala kapolo popeza zopulumukira kumakupatsani nthawi yochepa yofufuza kapena kupanga zosankha zambiri. Choonadi ndi chakuti, monga ndanena kale, nthawi zambiri anthu amapanga zitsimikizo zawo mozungulira cholinga chopeza kapena kusunga zofunikira. Amasiya chikhumbo chawo chofuna malipiro ndi masomphenya awo opeza zofunikira. Choonadi ndi chakuti takhala tikupanikizidwa kwambiri ndi malingaliro athu akupulumuka akugwira ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta kotero kuti tasiya kuzilota. Mantha amagwira maloto athu mu ukapolo, ndipo kusowa kwa zofunikira kumapangitsa maloto athu kukhala mu ndende ku zomwe sizingatheke.

Ndikukumbukira pamene loto langa linali loti ndikhale ndi ndarama zokwanira zogulira mafuta ondifikitsa kunyumba, osanena za zinthu zokhudza umoyo weniweni. Mmasiku amenewo, panalibe masomphenya a akulu mzofunikira zanga. Kungolipira cheke cha *rent* pamwezi kunanditengera kuganizira konse komwe ndidakatha. Ndikuvomereza kuti ndizovuta kuona momwe munapambanirapo kale pamene mukupanikizika posowa chakudya kapena mukakumana ndi zovuta zachuma.

Pamene Adamu anapereka Ufumuwo, dziko latsopano la imfa, mantha, kukhala ndi moyo, ndi nkhawa zitenga malo mmoyo mwake. Ndikukhulupirira kuti tonse tikudziwa momwe mantha amachitira. Ndikukumbukira nkhani zosawerengeka za mmoyo wanga wa nkhawa, manyazi, ndi mantha pamene ndinavutika mzaka zisanu ndi zinayi za chipwirikiti chandarama, potsirizira pake ndinalimbana ndi ziwopsezo za nkhawa, ndi kukhala ndi mankhwala ochepetsa kupsinjika maganizo. Kukhala mu dongosolo la temberero la dziko lapansi la kupulumuka kwatiphunzitsa tonsefe kukhala ndi kaonedwe koipa ka moyo. Ena amachita nako bwino

kuposa ena, koma popanda Kristu, malingaliro oipawa amatiuza mosalekeza kuti sindife abwino kwenikweni.

Kodi munayamba mwamvapo wina akunena kuti, “Musakhale ndi chiyembekezo?” Pokula, ndikasangalala ndi chinthu chimene bambo wanga anali kuganiza kuti ndi chopusa, anali kundiuza kuti, “Tsiku lina udzakula.” Chifukwa cha zimenezi, nthawi zambiri sindinali kulota chilichonse kupatulapo zimene bambo wanga anali kufuna. Ndikukhulupirira kuti bambo wanga anapwetekedwa chifukwa chokulira mu banja la uchidakwa, ndipo izi ndi zimene anafunikira kuchita pamene anali kukula.

Kunena zoon, tonsefe kuyambira pamene tinabadwa tkhala akatswiri a nkhawa. Mantha ndi chilankhulidwe chodziwika padziko lapansi. Ngati muima ndi kuganizira ichi, liwu lakuti *ayi* lakhazikika mwa ife kuyambira pamene tinabadwa. “Ayi, simungakhale nazo.” “Ayi, bwezerani zimenezo.” “Ayi, simungapite kumeneko.” “Ayi, simungakwanitse icho.” Pamapeto pake, timangosiya kunena kuti “Inde” ku china chilichonse kupatula kuthawira mwa apo ndi apo ku zochitika zomwe zimasokoneza malingaliro athu ku zochitika zathu zenizeni, monga kudya kopitirira chakudya chomwe timakonda kwambiri.

Kafukufuku wina amasonyeza kuti mwana wamba amamva mawu akuti *ayi* kapena *usachite* koposa 148,000 pamene akukula, poyerekeza ndi mauthenga mazana angapo a *inde*.⁴

Posachedwa ndidakhala ndi msonkhano wathu waukulu wapachaka, ndipo pa nsanga ndinaika Ferrari ya 2017, galimoto yoti isiriridwe ndithu. Koteru mwini wake wa galimotoyo amabwera kutchalitchi kwanga ndipo analipira ndarama zogulira galimotoyo, yomwe inali pafupifupi \$400,000. Pamene obwera onse anafika, anasirira ndi kuyang’ana galimotoyo, onse akuiyang’ana, kufuna

kufika pafupi. Koma ngakhale kuti onse anasirira galimotoyo, fundo imene ndinayiikira pa nsanja sinali kusonkhezera moyo wa zolinga za zinthu zakuthupi koma, mmalo mwake, kuwaphunzitsa phunziro. Anthu onse anasonkhana mozungulira galimotoyo, onse akunena kuti akufuna kuiyendetsa.

Ndinadziwa kuti maphunziro a “ayi” omwe adalandira mu ntchito ya zowawa komanso zokhetsa thukuta anali kufuula mosaz-indikira kuti, “AYI, sumudzakhalapo ndi galimoto yoteroyo! Ayi, simudzakwanitsa; musaganize nkomwe za iyo.” Chifukwa cha maphunziro ya “AYI” omwe anali nawo, ambiri aiwo sanaganizepo zokhala ndi Ferrari chifukwa malingaliro awo a ayi sanali kuona kuti adzakhala nayo. Komabe, ngati ndikanapitirizabe kusintha magalimoto ola lililonse, kuchoka pa okwera mtengo kupita ku otchipa kwambiri, potsirizira pake, ndikanakhala ndi galimoto pa nsanja imene iwo adakaganiza ndi kunena kuti, “Ndimakonda galimoto imeneyo; ndiyenera kukhala ndi imodzi yotere.”

Kodi pali kusiyana kotani? Zonse zinali monga momwe amadzi-onera, ndi mtengo wa galimoto. Inde, padakakhalapo ena amene akadati kwa iwo okha kuti, “Tsiku lina ndidzakhala ndi galimoto,” kapena analipo anthu amene anali ndi ndarama ndipo anaona galimotoyo mosiyana. Koma ndikutsimikiza kwa anthu ambiri, inali galimoto imene sinali ngakhale mmaganizo awo. *Millionaire* yemwe adapereka ndarama pa galimotoyo ali ndi theka la ma Ferrari. Mu maganizo iyi ndi galimoto yabwino. Pamene adaona galimotoyo, adaganiza kuti zoti ikhale yake anapitirira ndi njira yoitanitsira ku Italy, kuti itumizidwe ku mudzi kwawo ku US. Kunali kosavuta kuti achitepo kanthu pa masomphenya awa popeza anali nazo zokwanira. Nayi fundo yofunikira kuikapo mtima—kukhala ndi zofunikira ndi masomphenya-akutsogolo.

Fundo Yaikulu:

Kukhala ndi Zofunikira Ndi Masomphenya-akutsogolo

Popanda kukhala ndi zofunikira palibe masomphenya; pali kukhala ndi moyo kokha. Dongosolo la temberero la umphawi laba maloto athu ndi tsogolo lathu. Ndidziwa kuti Ferrari chinali chisonyezo chosayambekezera koma chinapanga kuti fundo yanga imveke. Anthu a kumeneko sanalole nkomwe kukhala ndi maloto okhala ndi galimoto ngati imeneyo chifukwa anaiona kuti ndiyosatheka. Ngakhale kuti akadayesera kulota, maphunziro awo a dongosolo la temberero la dziko lapansi likadawaseka. “Kutaya ndarama kotani!” Koma bwanji mudakakhala ndi ma *billion* makumi awiri ndi mphambu zisanu ku *bank* kwanu (ndikungotsimikiza fundoyi)? Galimoto ikadaoneka yosadula kuti mudakangogula imodzi yongogwiritsa ntchito pakutha kwa sabata. Ndi maonedwe chabe ndipo popeza Mawu a Mulungu amanena kuti lonjezo lililonse la Mulungu ndi “Inde” ndi “Amen (zikhale motero),” maonedwe anu ayenera kusintha kuti aganize monga momwe Mulungu amaganizira.

Pakuti monga mawerengedwe a malonjezano a Mulungu ali mwa Iye “Eya”. Chifukwa chakenso ali mwa Iye “Amen,” kwa ulemerero wa Mulungu mwa ife.

— 2 Akorinto 1:20

Malinga ndi mtanthauziramawu, kufotokoza kwa maonedwe ndi khalidwe lapadera ku njira yokhudza chinachake: fundo ya kaonedwe, khalidwe, cholozera, kapena kutanthauza. Chachikulu, maonedwe ndi momwe kwenikweni muganizira za chinthu chake.

Nawu mchitidwe umene ndikufuna muganizire. Adamu anali kalonga asanagonje kwa Satana. Kotero ngati mukadamuona pambuyo pake atachimwa, mudakaona munthu wosauka ndi banja losokonezeka (Kaini, mwana wake, anapha mbale wake, Abele), ndipo simukadampatsa mwayi wakukhala winawake. Koma chimene simunachione ndi chakuti anali ndi ufumu kwa omtsatira ake. Ngakhale simudamuone pa udindo umenewu, analengedwera kulamula ndi kulamulira mmoyo. Choonadi chomwecho chigwira ntchito kwa inunso. Simungangodziyang'ana nokha potengera komwe mukukhala, zomwe muli nazo, momwe zanu ziliri panopa, ndikuyesa luso lanu. Muyenera kuyang'ana paluso lanu.

Ndikutha kukumbuka momwe ndinali mzowawa, ndipo ndimakumana ndi zinthu zazikulu zoposa ineyo. Ndidayenera kuchita zitsimikizo zimene zidakatenga ndarama zimene ndinalibe. Ndinamva zomwe Mulungu amandiuza kuti ndichite, koma ndinali wamantha pang'ono chabe kulumphiramo. Ambuye anandipatsa loto pa nthawi imeneyo. Ndinali pa kavalo pa mwamba pa phiri. Ndinali ndi lupanga mmanja mwanga. Pansi pa ine mmunsi mwa phiri munali anthu mazanamazana, kapena zikwizikwi, za adani okwera pa akavalo ndi malupanga awo anandiukira. Ndinali ndekha pa phiripo ndipo iwo anali ochulukadi. Liwu mloto langa linanena mawu awa, “Usadzichepetse wekha, Gary!” pamenepo, ndinakweza lupanga langa ndikuyamba kuthamangitsa kavalo wanga kutsika pa phiripo kupita kwa adani amene ataona mphamvu zanga, nawonso anatenga zawo mphamvu, kukwera ku

**MAONEDWE ANU
AYENERA KUSINTHA
KUTI AGANIZE MONGA
MOMWE MULUNGU
AMAGANIZIRA.**

phiri kumene ndinali atakweza malupanga awo. Pamene ndinathangira kwa iwo, ndinafuula mokweza, “*THOR!*”

Nditadzuka, ndinadziwa kuti Ambuye anali kulankhula kwa ine ndikundilimbikitsa, koma sindinadziwa liwu lakuti *Thor* kuti limatanthauza chiani. Ndili ndi munthu mtchalitchi yanga amene wakhala mbusa kwa zaka makumi atatu ndipo anaphunzira zilankhulidwe zosiyanasiyana. Ndinamufunsa ngati akudziwa zimene liwuli limatanthauza ndipo anafufuza. Tsiku lotsatira anandiimbira foni nati Thor litanthauza mwana wabingu. Ndinamuthokoza ndipo ndinadabwa ndi chimene Ambuye anandiuza. Kwa adani, ndinamveka ngati bingu! Pokhapokha nditamuuza mdyerekezi za kufooka kwanga, pamene ndilankhula, zimveka monga bingu (mphamvu) kwa iye.

Ndinali kulalikirira ku Msonkhano woyamba wa Zofunikira mu 2010 ndipo ndimanena nkhani ina. Polumikiza nkhaniyo, ndinamaliza ndi kunena zimene Yehova anandiuza mmaloto, “Pamene mdani akuona ukubwera, Gary, umamveka ngati bingu.” Nthawi imeneyo ndinati, “Zikumveka ngati bingu,” kugunda kwa bingu kunadzaza kumwamba. Kunalibe mvula, kunalibenso bingu lina mmbuyomo, ndipo kumeneko kunali kugunda kokhako kumene kunamveka usiku onse. Anthu amene analipo usiku umenewo anadabwa. Koma panalibe amene anali osangalala kwambiri koposa ine, monga ndinadziwa kuti anali Ambuye akuika, “AMEN” Wake pa zimene ndimanena monga zinakhudza ana Ake onse. Komanso, makamera a *TV* anali kujambula usiku umenewo, ndipo ngati mufuna zimenezo mukhoza kuziona pa: <https://youtu.be/rtx1XYJGIAg>.

Kotero pano ulipo mchitidwe umene muyenera kumvetsa.

Akapolo salota maloto a akulu!

Kodi akapolo amalota chiyani? Kuimitsa, ndicho chiyani. Amalota za ola la 5:00 pamene akuyang’ana mawotchi awo mkati mwa theka lachiwiri la tsiku, akufuna kuima ndi kusiya ntchito. Amalota za tchuthi, amalota zopuma pantchito, amalota atakhala ndi ndarama kuti asiye ntchito. Akapolo amalota za kusiya, osati kupanga ntchito zina zambiri! Malingaliro aukapolo kapena maonedwe samangoyambitsa kapena kupanga ntchito; koma njira yochokera pa ntchito. Kapolo amakhala wotopa kale ndipo saona luso limene lingamuthandize tsiku lililonse.

Kuti mukhale mutu osati mchira, malingaliro anu ayenera kusintha kuchoka ku ukapolo kupita ku mwini wake ndi mlengi. Muyenera kuyambanso kulota. Muyenera kuyang’ana kumbuyo zomwe mukuganiza kuti ndinu ndani, chifukwa ngakhale mutha kuoneka wofooka mmaso mwanu, kwa mdyerekezi mumamveka ngati bingu. Muli ndi magazi achifumu mmagazi anu, ndipo mumangofunikira kuganiza ndi kuchita monga choncho.

Ndili ndi mnzanga yemwe ndi wopeza ndarama zambiri. Iye ali ndi nyumba zambiri zokongola, zonse pa mnyanja. Tsiku lina pamene ndinali kumuona, tinali kuyenda padoko pakati pa ngalawa. Tikamadutsana anali kuitana aliyense mwini wake. Ndikukupatsani chitsanzo cha momwe zokambiranazo zidamvekeru, koma ndikungoyerekeza maina, popeza sindiwakumbukira. Chifukwa chake zokambirana za mnzanga zidamveka motere: “Ngalawa iyi ndi ya Billy Smith, yemwe ali ndi *Ohio Medical Services*. Ngalawa yotsatirayi ndi ya John Rogers, yemwe anali mwini wa *firm* yotchedwa Rogers and Rogers ya za malamulo. Ngalawa yotsatira iyi ndi ya Ralph Tidewell, yemwe ali ndi sitolo yabwino ya nsapato pa High Street.”

Pamene tinali kuyenda pamzere wa ngalawa, ndipo nditadutsa pafupifupi makumi awiri a izo, ndinazindikira kuti iliyonse inali ya munthu amene anali ndi malonda. Palibe ngalawa ngakhale imodzi yomwe inali ya munthu monga Joe yemwe amagwira ntchito kuyambira 9 mmawa mpaka 5 madzulo ngati wantchito pamalo ogulitsira *ice-cream*. Tsopano, sindikutsutsa kugwira ntchito pamalo ogulitsira *ice-cream* ndipo sindikutsutsa kukhala wantchito. Ndikungokupatsani chitsanzo cha anthu omwe ali ndi chuma.

Chonde tcherani khutu ku zimene ndikunena. Sizokhudza ndarama zomwe ali nazo; ndi za malingaliro omwe ali nawo. Osapeza ngolo musanapeze kavalo. Anthu ambiri anganene kuti, “Ndikadakhala ndi ndarama zotere.” Zomwe amayenera kunena ndi “Ndikadakhala kumaganiza momwe amachitira.” Iwo ali ndi kaonedwe kosiyanana pa moyo ndi kaonedwe ka iwo eni.

Mabanja ambiri sapeza ndarama zomwe zioneka ngati zambiri. Kafukufuku waposachedwa akuti 51% ya ogwira ntchito aku America amapanga ndarama zosakwana \$30,000 pachaka. Oposa theka la dziko lathu amapanga zosakwana \$30,000 pachaka! Ngati muli ndi zaka makumi awiri ndikungoyamba kumene kapena muli paudindo chifukwa mukufunadi kukhalapo, ndipo ndarama sizili pamwamba pa mndandanda wanu ndi chabwino, koma ndikudziwa kuti sizoono kwa oposa theka la fuko lathu. Ndikudziwa kuti amafuna ndarama zambiri. Ndikhulupirireni, ndakhala mnyumba zambiri pazaka zanga za 36 ndili mu *macompany* azachuma, ndipo ndadzionera ndekha.

Nanga bwanji alibe ndarama zambiri? Musanayambe kufuula momwe moyo uliri wopanda chilungamo kapena momwe muli wozunzidwa kapena opanda pake, ndidzakupatsani zifukwa ziwiri. Choyamba, iwo ali mumsampha wa dongosolo la temberero la dziko lapansi la umphawi ndipo sadziwa za Ufumu wa Mulungu ndi fundo

Zake za kukhala ndi zofunikra. Chachiwiri, ali ndi malingaliro oipa, chifukwa cha maphunziro otembereredwa a dziko lapansi amene analandira, ndiponso chifukwa chakuti saona njira yotulukiramo, ngakhale kuti njira yina ili pamaso pawo. Kwenikweni, akapolo ali ndi malingaliro aukapolo, monga momwe ndakhala ndikunena. Iwo saona mwayi pamene akufuna mpumulo. Tiyeni tinene zoon; popanda mayankho enieni, anthu amataya mtima.

Ndiloreni ndikupatseni chitsanzo chomwe ndimagwiritsa ntchito mmaphunziro anga. Tiyerekeze kuti ndakuuzani kuti nditha kuthetsa mavuto anu onse azandarama mchiganizo chimodzi chophweka. Konzekerani pensulo ndi pepala lanu chifukwa ndikukutsimikizirani kuti ili likhala yankho lanu. Mwakonzeka? Chabwino, ndi izi: pangani ndarama zokwana \$5 *million* chaka chino. Ndikanena zimenezi kuchokera pa nsanja, aliyense amayamba kuseka. Koma ndi chifukwa chiyani amaseka? Chifukwa chakuti sangadzione okha akupanga ndarama zoterozo, kapena samalingalira kuti ndi zotheka kupeza ndarama zokwana \$5 *million* pachaka.

Kenako ndikuwauza kuti sadzakhala nazo zomwe sangazione. Kenako ndibwereze kunena, koma nthawi ino motsitsa nambala: \$200,000, \$100,000, \$70,000, kapena \$40,000 pachaka. Pamapeto pake, ndiwauza kuti, “Ndifika ku nambala yomwe mudzati, ‘Chabwino, zosavuta. Ndikhoza kuchita zimenezo.’”

Kenako ndiwauza nkhani ina. Tinene kuti ndine wamalonda wolemera wotumiza zinthu kunja. Ndikufuna kutumiza mipira ku China, ndipo ndikufuna thandizo lakulongedza kuti nditumize. Ndiwauza kuti ndiwalipira \$500 pa mipira uliwonse womwe aulongedze. Pongoganiza kuti atha kulongedza mipira mazana awiri patsiku, izi zingawapezere ndarama zokwana \$100,000 patsiku. Ndikufunanso kuwapatsa pangano la ntchito la chaka chimodzi yolongedza mipira

pamlingo womwewo. Tsopano, ngati ine ndikanati yankho lawo linali kupanga ndarama zokwana \$5 million mmiyezi khumi ndi iwiri, kuyankha kwawo kukanakhala kotani? “Zosavuta, palibe vuto, mutha kupanga \$5 million mosavuta.”

Kodi panali kusiyana kotani? Dongosolo, la zonsezo. Dongosolo limapanga kusiyana konse. Mulungu amene anakupangani akudziwa dongosolo, ndipo chimene mukusowa ndi kulimva. Ndi mmenenso ziliri ndi Ufumu wa Mulungu. Pamene Mulungu anandipatsa loto limenelo kuti ndiyambe malondayo ndi kundisonyeza mmene ndinga-chitire, ndarama zimene ndinali kupeza zinali zisanasinthe—koma ndinali kufuula mkati kuti, “Izi nzosavuta! Mavuto anga azachuma atha; Ndili ndi dongosolo!”

“Pakuti ndikudziwa malingaliro amene ndilingaririra inu,” ati Yehova, “malingaliro a mtendere, si a choipa, akukupatsani chiyembekezo ndi tsogolo.”

— Yereimiya 29:11

Mulungu ali ndi malingaliro akukulemeretsani! Mukangozindikira kuti Mulungu ali ndi dongosolo la kulemera kwanu, nkhondo yakhala pang’ono kutha! Mvetserani, kukonza zinthu zandarama sizovuta. Kukhala ndi zofunikira ndi masomphenya akutsogolo! Ndizosavuta kwambiri. Yankho losakhala ndi zakudya ndi kukhala ndi zakudya. Yankho pa chosowa cha nyumba yaikulu ndi chosowa nyumba yaikulu. Yankho la galimoto yodalirika ndi kukhala ndi galimoto yodalirika.

Ndikudziwa kuti ndikulankhula ndi zinthu ziwiri pano, koma ndinayendetsa galimoto yowonongeka kwa zaka zambiri. Mumatha kundiona ndikubwera pamtunda chifukwa ndimasiya utsi kulikonse

komwe ndinapita. Ndikudziwa momwe zovuta zamagalimoto zimakhalira mukafuna kupita kwina kwake. Ndikudziwanso momwe zimakhalira kulowa mmalo ogulitsa magalimoto ndikulipira ndarama zogulira galimoto yatsopano. Ingoganizani? Palibenso nkhwawa, palibenso kupsinjika. Chifukwa chiyani? Chifukwa chosowa changa

**MONGA NZIKA YA UFUMU,
MULI NDI UFULU WA
ULAMULIRO, NDIPO
LAMULO LILILONSE
NDI FUNDO ILIYONSE
TSOPANO NDIYOPEZEKA
KWA INU.**

chakwaniritsidwa ndipo ndili ndi mtendere. Ndikhoza kuyang'ana pa chimene ndiyenera kumachita mmalo molimbana ndi mavuto agalimoto.

Choonadi cha chinthu ndi kuti anthu ambiri ayenera kuchita ndi zinthu za ndarama zenizeni mpaka ukhala pa opsinjika nthawi zambiri za miyoyo yawo. Akhoza kumagwira ntchito maola ambiri kuyesetsa kuti apeze koma alibe moyo weniweni. Mnzanga, ichi sichifuniro cha Mulungu pa moyo wako.

Monga ndanenera kale, anthu amasiya maloto awo ndi zikhumbo zawo za malipiro pa ntchito zomwe amanyoza. Akapolo nthawi zambiri sianthu osangalala! Tsoka ilo, kuno ndi kumene anthu aliri, osakondwa ndi kumene aliri mmoyo, onyansidwa, ndi opanda chiyembekezo. Koma zoonza zake nzakuti ali pafupi ndi maonekedwe akusinthira ku ufulu kapena, monga ndagawana nawo, kukhala ndi dongosolo.

Ndiloreni ndikupatseni chitsanzo changa. Ambiri a inu mukudziwa kuti ine ndimakonda kusaka ndi kusodza, kukwera njinga ndi kukwera mapiri, chilichonse chochitikira kunja. Ndinakulira ku Ohio mu dera la laling'ono la alimi lomwe

limadziwika kuti *Plain Township*. Linali kitchedwa *Plain Township* chifukwa, monga momwe mungaganizire, linali lopanda mapiri. Inde, zimenezo zinali zabwino kwa alimi, koma sanali malo ogwira mtima kwambiri. Ndidalipira ku *magazine* iliyonse yosaka ndi yosodza monga ndikadathera, *Outdoor Life*, *Sports Afield*, *Field & Stream*, ndi ena. Ndidakhoza kuwerenga nkhani zazikulu za kusodza ndi kusaka mmapiro akutchire ndi okongola kumadzulo ndi mapiri obiriwira a Appalachian Valley ola limodzi chabe kummawa kwanga. Komabe sindinapiteko kumadera amenewo. Ndinali ndi zaka makumi anayi ndisanaone phiri langa loyamba.

Chifukwa chiyani? Ndinali ndi ndarama zoyendera, ndinali ndi galimoto yangayanga, *Interstate I-70* imadutsa kumudzi kwathu, ndipo imapita kumadzulo kudutsa kumapiri a Rocky. Koma choonadi chake ndichakuti sindinaganizepo zopita kumeneko kapena kudzilola kuganiza kuti, “Ndidzapitako tsiku lina.” Ndinali kusirira malowo chifukwa cha zithunzi zonyezimira za *magazine* koma sindinaganize zopitako. Zikadakhala zosangalatsa monga momwe zinandikhudzira; koma sizinali zotheke mu maganizo mwanga. Pamene ndinali ndi zaka makumi anayi ndipo pomalizira pake ndinapita kumadzulo, sindinakhulupirire zimene ndinataikiridwanazo mmoyo wanga wonse. Tsopano, ndiyenera kukwera phiri kosachepera kamodzi pachaka. Mnzanga, kuli zambiri kunja uko kuposa zomwe mukuziona pakali pano. Ndinu oposa zomwe mukuona pakali pano! Pali maonedwe osiyana ku moyo amene mufuna kuona ndi kulawa.

Pamene muyamba kumvetsetsa ndi kuphunzira mmene Ufumu wa Mulungu umagwirira ntchito ndi zimene Ufumu wa Mulungu umanena kuti muli nazo kale, kaonedwe kanu kadzasintha!

Pamenepo, ndipo simulinso alendo ndi ogonera, komatu muli a mmudzi womwewo wa ojera mtima ndi a banja la Mulungu.

— Aefeso 2:19

Monga nzika ya Ufumu, muli ndi ufulu wa ulamuliro, ndipo lamulo lililonse ndi fundo iliyonse tsopano ndiyopezeka kwa inu. Ili linali vuto la Drenda ndi langa. Ngakhale tinali Akristu komanso okonda Mulungu, tinali mbadwa za Ufumu wa Mulungu osadziwa malamulo ndi fundo za Ufumuwo. Chifukwa cha kaonedwe kathu kocheperako kamene dongosolo la temberero la dziko lapansi linatipatsa, tinalibe maloto. Koma chidziwitso ndicho mphamvu.

Mwachitsanzo, mubwalo lamilandu, pangano losainidwa la *rent* limatsimikizira kuti muli ndi ulamuliro wokhala mnyumba mwanu. Chidziwitso chakuti chilipo chikalata chosainidwa ndi mwayi wopeza chilungamo kuti mutsimikizire kuti muli ndi ulamuliro wokhalira mnyumbayo kumakupatsani mtendere ndi chithonhozo. Chimodzimidzi, chidziwitso cha zimene Mulungu amanena ndi zimene Ufumu ukusungirani kumakupatsani chidaliro cha kutenga chilichonse chimene chili chanu mwa ulamuliro. Mwachitsanzo, kodi kulemera kwa mlimi ndi chiyani? Ndi ndarama? Ayi. Kodi ndi mbewu imene amafesa? Ayi. Ndi chidziwitso chimene iye ali nacho cha malamulo a kufesa ndi kukolola. Ngakhale atakhala wosauka

chotani, iye amadziwa mmene angakhalire wolemera. Amangotsatira pa malamulo a dziko lapansi amene Mulungu anakhazikitsa. Njira yobzala ndi kukolola imatha kuberekeramlimi mobwerezabwereza.

Iye amamvetsa malamulo okolola ndipo amawadalira kwambiri. Iye anafesa mbewu zamtengo wapatali za madola zikwi zambiri mu nthaka, komabe sachita mantha. Simudzapeza mlimi atakhala pafupi ndi *tractor* yake atabzala mbewu yake akulira za ndarama zonse zomwe waponya pansi. Ayi, sakanalira chifukwa cha mtengo wa mbewuyo. Adzakhala ndi chidaliro cha malamulo okhudza chilengedwe cha dziko lapansi. Kodi angakuuzeni mmene mbeu imamerera? Ndikukaika, koma angakuuzeni kuti akufunafuna malo ena oti alime. Chimodzimodzinso ndi inu ndi ine. Tikapanda kudziwa malamulo a Ufumu ndi kuwadalira, sitingasangalale ndi moyo umene Mulungu watikonzera.

Imodzi mwa nkhani zosangalatsa kwambiri ndi imene tinachitira umboni mmasiku oyambirirawo pamene ndinalandira foni kuchokera kwa mwamuna amene ndidzamutcha kuti “Don,” amene anali ndi mavuto aakulu azachuma. Iye anali atamva kuti ndidathandiza anthu pa chuma chawo.

Pamene ndinakumana ndi Don, anabwera ku ofesi yanga wokhumudwa kwambiri komanso anali ndi ngongole. Palibe chimene chinkaoneka kuti chikuyenda bwino mmoyo wake panthawiyo. Nditakhala pansi ndikulankhula naye, ndinapeza kuti anali miyezi itatu kapena inayi kumbuyo polipira *rent* yake komanso pafupifupi anali kumbuyo polipira ngongole zonse zomwe anali nazo. Panali mavuto a mu banja—mkazi wake anali atatopa ndi mavuto awo a zachuma ndipo anayamba kuleka kulemekeza Don, amene anali kulephera kupezera banja lake zofunika pa moyo ndi ana awo asanu. Zoonazake ndi zakuti zinthu zinaipira Don. Ndipo anali ndi mafunso ambiri.

Ntchito yake inali yogulitsa *health insurance* kudera lonse la Ohio, koma kusachita bwino kunamufikitsa pamavuto a zachuma.

Ngakhale kuti panali zinthu zambiri zoipa za Don, ndinaona kuti angathe kuchita bwino pa zimenezi. Anali wofunitsitsa kuphunzira ndi wofunitsitsa kugwira ntchito. Kuphatikizika kwamphamvu kumeneku kunandichititsa chidwi kwambiri kuti ndimulembe ntchito ndikudziika ndekha mzokhudza umoyo wake wa kutsogolo. Pamapeto pake, kunali komwe kunapereka phindu lalikulu kwa tonsefe.

Company yanga yatsopano inali itangopeza mwayi wa ulendo wopita ku Hawaii kuchokera kwa mmodzi wa ogulitsa athu, ndipo ndinalingalira kuti uwu ukakhala mwawi waukulu wogawana ndi Don ponena za Ufumu wa Mulungu. Ngakhale kuti anali Mkristu, sankamvetsa zinthu ngati mmene ndinkamvera. Ndipo ngakhale kuti ndinayesetsa kangapo kumuuzza fundo za Mulungu pa nkhani imeneyi, ankangooneka kuti sankakhulupirira zimene ndimanena.

Ndinapitiriza kufunafuna njira yokopa chidwi cha Don imene ikanamthandiza kuzindikira kuti nayenso akhoza kukhala ndi chipambano mwa kuphunzira mmene Ufumu wa Mulungu unagwirira ntchito. Komabe anavutika kuti adzikhulupirire komanso kukhulupirira kuti kusintha kungachitikedi. Ndinadziwa uwu ulendo wa ku Hawaii unali mwayi wanga.

Kutatsala milungu ingapo kuti tipite, tinakambirana zimene tikaone ndi kuchita kumeneko. Chidwi chimodzi chapadera chinagwira Don kuposa china chilichonse. Ankafuna kugwira nsomba *yablue (blue marlin)* mmadzi okongola a mu Pacific. “Hawaii ndi likulu la nsomba zoterezi padziko lonse lapansi,” Don adandiuza mokondwera. “Nthawi zonse ndakhala ndikufuna kugwira nsomba imeneyi; lakhala loto langa.” Kwa nthawi yoyamba

mmasabata angapo, ndinaona kuwala mmaso mwa Don. Chinachake chimamukondweretsa, ndipo ndinadziwa kuti chisangalalo chake chidzatsekula chitseko cha phunziro lamphamvu.

“Don,” ndinatero, “kodi umadziwa kuti ndikotheka kudziwa, osati kuyembekeza, koma *kudziwa* kuti ukagwira nsombayi ku Hawaii polowa mu Ufumu wa Mulungu?” Mosokonezeka koma mochita chidwi, anafuna kudziwa zambiri, ndipo ndinapitiriza kufotokoza za Ufumu. Ndinagwira mawu apa Maliko 11:24, imene imati: “*Chifukwa chake ndinena ndi inu, zinthu zilizonse mukazipemphera ndi kuzipempha, khulupirirani kuti mwazilandira, ndipo mudzakhala nazo.*” Kwa Don, izi zinali zabwino kwambiri kuti azikhulupirire. Ndinatenga nthawi kuti ndimuthandize kumvetsa za Ufumu ndi mmene angamasulire chikhulupiro chake. Ndipo kotero, tisananyamuke pa ulendo wathu, iye ndi mkazi wake anafesera monga momwe ine ndinachitira kwa gwape wanga, anapemphera mogwirizana, ndipo anakhulupirira kuti iwo adzalandira nsombayi (*blue marlin*).

Pa nthawiyi, Don nachita zonse zimene ankadziwa kuti agwire ntchito yokololayi. Anachita kafukufuku pa mabwato omwe analipo ndi mitengo yabwino ndipo potsirizira pake anasungitsa malo ndi woyendetsa amene adamukonda. Chilichonse chinakhazikitsidwa, ndipo tonse tinali okondwa kwambiri kupita kumadzi a *blue* aku Hawaii.

Tsiku lolowa mmadzi linafika, ndipo pamene tinali kukwera bwato, tinauza kapitawo mosangalala kuti lero ndi tsiku lomwe tigwire nsomba ija. Ngakhale kuti ankayembekezera kuti tsiku lililonse tizidasodza nsomba zina, iye anatitsimikizira kuti siinali nyengo yabwino yoti tigwire nsomba yotere tsiku limenelo. Pokhala ndi mabwato awiri paulendo wokonzekedwa tsiku lililonse

kwa miyezi inayi yapitayo, antchito ake anangobweretsa nsomba yamtundu uwu (*blue marlin*) imodzi. Izi zidachitika makamaka chifukwa choti sinali nyengo yake yakusodza nsomba zotere, chifukwa inali nsomba yosamukasamuka. Pokana kuti tikhumud-witsidwe, tinamuuzwa mwaulemu kuti tidzalandira imodzi ndipo tinapitiriza kukonza zida zathu.

Titayenda kwa maola asanu ndi limodzi tikusodza, sitinagwire chilichonse, ndipo ndinayamba kuda nkhwawa kuti kusachitapo kanthu kungafooketse chikhulupiriro cha Don. Mukudandaula kwanga ndinamufunsa funso. “Don,” ndinafuula ndili pamlatho womwe unali pamwamba pake, “ndiloreni ndikufunsemi funso. Ndi liti pamene munalandira nsomba ija, pamene anaonekera kapena pamene tinapemphera? Molimba mtima, anayankha mwamphamvu kuti, “Gary, nzosavuta. Ndinalil-andira pamene ndinapemphera.” Ndinasangalala kwambiri nditamva yankho lake. Apa ndi pamene ndinadziwa kuti Don analabadira malangizo anga ndipo anatsimikiza mtima kulandira nsomba imeneyo.

Patangopita mphindi pang’ono, mbedza ya Don inali kulowa mnyanja ndipo anzakewo anakuwa, “Nsomba!”

“Musakondwe kwambiri,” anachenjeza woyendetsa. “Ndi nsomba yaikulu, koma si *blue marlin*. *Marlin* zimabwera pamwamba ndikudumpha modabwitsa mumlengalenga, ndipo nsombayi imakhala kozama.” Nthawi inatha pamene Don anapitiriza kulimbana ndi nsomba yomwe inali isanayandikire kumtunda kuti iwoneke. Ngakhale kuti Don anali wotopa, nsombayo inali yotopanso ndipo posakhalitsa idasiya kulimbalimba. Don ndi ine sitinadabwe pamene *blue marlin* yaikulu inaonekera, nsomba yokongola ija, koma aliyense mu bwatomo anadabwa.

Chithunzi cha Don ndi nsomba yake chidakali mu ofesi yanga mpaka lero monga umboni kwa ena ndi chikumbutso chosalekeza kwa ine cha chenicheni cha Ufumu. Kunja inali nsomba chabe. Koma kwa Don, *marlin* inkatanthauza zambiri. Ngati Ufumu unagwira ntchito kwa *marlin*, ndithudi ukanathandiza china chilichonse chimene iye anafunikira mu umoyo. Kwa Don, kunali kuyamba kokha kwakuzindikira ndi kukhudza kumene Ufumu wa Mulungu unachitira pamoyo wake.

Ndimakonda nkhani imeneyi, ndipo ndimakonda kuona anthu ali ndi maonekedwe enieni a Ufumu wa Mulungu. Ichi ndi chimene ndifunanso kwa inu!

MUTU 4

NDINAPEZA FUNGULO YAIKULU YA UFUMU

Tonsefe tili ndi mafungulo a mitundu yosiyanasiyana ya nyumba zathu, galimoto zathu ndi chilichonse tifuna kutchinjiriza. Fungulo itipatsa mwayi ndi ulamuliro kuti chotchinjirizidwa mkati tichigwiritse ntchito, monga galimoto. Monga Mkristu pokhala zaka zisanu ndi zinayi mmavuto achuma opanda chiyembekezo, ndinadziwa kuti china chake chikusoweka, china chake chinali cholakwika. Palibe amene anganayenera kundiuza zimenezo. Chimene ndidayenera kudziwa ndi chakuti chinalakwika ndi chiani ndi makonzedwe ake.

Pamene Yehova analankhula kwa ine polirira chithandizo kwa iye, nditagona pa bedi ku kanyumba kophwanyika ka ku famu, anandiuza kuti vuto langa inali lakuti sindinaphunzire momwe Ufumu Wake umagwirira ntchito. Mu fundo imodzi imeneyo ndinamva fungulo, kapena ndinene kuti gwero la fungulo kapena mafungulo ofunikira—Ufumu. Mulungu amandiuza kuti yankho langa linali mu Ufumu Wake. Ndinali ndisanaphunzire kuti Ufumu Wake umagwira ntchito bwanji, ngati ndinatero, ndikadapeza

yankho. Pamene Mulungu analankhula kwa ine zakusowa chidziwitso changa cha Ufumu, ndinalibiretu ganizo kuti Amatanthauza chiani za Ufumu. Koma ndinamumva momveka kuti ndidakaphunzira momwe Ufumu Wake umagwirira ntchito ndikapeza mayankho amene ndimawafuna. Tsono kwa ine, fungulo yaikulu inali mu ndemanga imeneyo, “Sunatengepo nthawi yophunzira momwe Ufumu wanga umagwirira ntchito!” Inde, ndemanga mwa yokha inanena zambiri ndipo zoonadi, fungulo yanga yoyamba ku moyo wanga inali kusinthidwa.

Pakuti kwa ife mwana wakhanda wabadwa, kwa ife mwana wamwamuna wapatsidwa, ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lake. Ndipo adzatchedwa Wauphungu Wodabwitsa, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha, Kalonga wa Mtendere. Zakuonjezera ulamuliro wake ndi mtendere sizidzatha. Iye adzalamulira pampando wachifumu wa Davide ndi Ufumu Wake, kuukhazikitsa ndi kuuchirikiza ndi chiweruzo ndi chilungamo kuyambira nthawi yatsopano ndi kunkabe nthawi zonse. Changu cha Yehova wa makamu chidzakwaniritsa zimenezi.

— Yesaya 9:6-7

Kumvetsetsa kuti Ufumu wa Mulungu ulidi ufumu umene umagwira ntchito pamaziko a boma ndi malamulo kunanditsegu mmaso kuti ndimvetsetse Ufumu umene ndinali ndisanaudziwe. Kudziwa kuti Ufumu wa Mulungu unakhazikitsidwa ndipo ukuchirikizidwa ndi chilungamo (kayendetsedwe ka malamulo) ndi chilungamo cha Mulungu (malamulo Ake) kunandisonyeza kuti chilichonse chimene chimachitika mu Ufumuwo

chimachitika chifukwa cha lamulo kapena fundo ya Ufumuwo. Mwina sindingakhale wanzeru kwambiri pa gulu, koma ndinali wanzeru mokwanira kumvetsetsa kuti ngati Ufumu umagwira ntchito pamaziko a malamulo ndiye kuti ndikhoza kuphunzira malamulo amenewo ndi kuwagwiritsira ntchito mmoyo wanga. Pamene Mulungu anayamba kuvumbulutsa ndi kuphunzitsa Drenda ndi ine malamulo Ake, ndinayamba kuzindikira kuti nkhani iliyonse ya mu Baibulo inali ndi mafungulo amene ndinafunikira kudziwa momwe Ufumu umagwirira ntchito. Ndinayamba kuwerenga nkhani iliyonse ya mu Baibulo mosiyana: “Ndi chifukwa chiyani zimenezi zinachitika? Chifukwa chiyani sizinachitike?” Ndinali kuwerenga nkhani iliyonse ndi maganizo akuti, “Kodi ndi fundo ziti zimene zavumbulutsidwa mu nkhaniyi? Zinachitika bwanji?”

Ndinayamba kudziticha katswiri wauzimu, ndipo ndinali wokondwa pamene Mzimu Woyera unandiululira malamulo. Ndinasangalala kwambiri kuona kuti malamulo amene ndinapeza atha kugwira ntchito pa moyo wanga monga momwe amachitira mu Baibulo. Anthu amandifunsa kuti, “Gary, ukutanthauza chiyani ponena za malamulo a Ufumu?” Nthawi zambiri ndimawakumbutsa malamulo onse amene amagwiritsa ntchito padziko lapansi pano—mphamvu yokoka, malamulo a *physics* ya zinthu zachilengedwe, ndiponso malamulo onse okhudza chilengedwe.

Mlimi amagwiritsa ntchito malamulowa nthawi iliyonse yomwe akufuna; sayenera kuwapempherera kuti agwire ntchito. Amagwira ntchito nthawi iliyonse yomwe amasankha kuwagwiritsa ntchito. Amapezeka kwa aliyense komanso aliyense amene akufuna kuwagwiritsa ntchito. Mofanananso, Ufumu wa Mulungu umagwira ntchito ndi malamulo amene tingaphunzirepo. Popeza iwo ndi

malamulo, sasintha, ndipo angaphunzitsidwe ndi kugwiritsidwa ntchito ku moyo mu Ufumu.

Momwemonso, mukabwera kwa Kristu, ndinu mbadwa ya Ufumu Wake, ndipo Ufumu wonse ndi wanu. Malamulo awa a

**PAMENE MULUNGU
ANAYAMBA
KUVUMBULUTSA NDI
KUPHUNZITSA DRENDA
NDI INE MALAMULO
AKE, NDINAYAMBA
KUZINDIKIRA KUTI NKHANI
ILİYONSE YA MU BAIBULO
INALI NDI MAFUNGULO
AMENE NDINAFUNIKIRA
KUDZIWA MOMWE UFUMU
UMAGWIRIRA NTCHITO.**

Ufumu mungawaphunzire ndi kuwagwiritsanso ntchito.

“Chabwino,” anthu adzandiuza, “Ndamvetsetsa gawo lake, koma ndipatseni chitsanzo cha lamulo mu Ufumu.” Pali malamulo ambiri, ambiridi. Kunena zoonā, ndalemba kale koma owerengeka, monga lamulo la mphamvu ya ulamuliro, lamulo lachikhulupiriro, ndi lamulo la mgwirizano, ngakhale kuti sindinatuluke poyera ndikuwacha monga mmitu yoyambirira. Apanso, pali malamulo ambiri, ndipo malamulo onsewa akhoza kugawidwa kukhala ntchito ndi kugwiritsidwa ntchito, omwe

ali magawo amene tifuna kuwaganizira. Ndiloreni ndikupatseni nkhani kuti ikuthandizeni kufotokoza zomwe ndikunena.

Ndili ndi ndege, *Piper Mirage*, yomwe ndimagwiritsa ntchito popita kumisonkhano, kukumana ndi ogulitsa, komanso kuyenda ku zamalonda. Ndinakonzekera ulendo wopita ku Colorado kukachita nawo msonkhano ndipo ndinali nditakonzekera mosamalitsa zofunikira za malamulo paulendowu. Ngati simukudziwa, ndege iliyonse yomwe imawulukira ku U.S. imayenera kupereka

lipoti la masungidwe ndi kukonzedwa kwake kamodzi pa chaka. Woyendetsa ndege wanga anayenera kukatenga Mirage ndikutipititsa kumsonkhano wathu. Koma kutatsala tsiku limodzi kuti atitenge, akusitolo anaimba ndi kunena kuti mwangozi anathyola galasi lakutsogolo la kwa woyendetsa ndegeyo. Iwo adzabwezera lina mmwaulere, koma kukonzaku kudzatenga masiku atatu ndegeyo isanakhale bwino. Izi zinatanthauza kuti ine ndi Drenda tinayenera kukakwera ndege ina yolipira kupita ku Colorado. Mosaganizira zosadandaula, koma nthawi zonse timakonda kuyendetsa ndege yathu kulikonse komwe tingapite ngati tingathe. Tinakhumudwa pang'ono koma tinapita ku msonkhano. Cholinga chake chinali chakuti woyendetsa ndege wathu adzatinyamule ulendo wobwerera ku Ohio.

Patangotha masiku awiri msonkhano wathu uli mkati, kunagwa matalala mwadzidzidzi. Matalalawo anali aakulu kwambiri moti anawononga dera lonselo. Mmadera ena, tinthu tambirimbi ta *ice* tinaboola madenga. Magalimoto ambirimbi anawonongeka osakonzedwanso. Nyumba ndi madenga zinawonongeka. Pamene woyendetsa ndege wanga anabwera kudzatitenga, anaimika pa FBO yomweyo imene akadaiika tinganabwera nayo koyambirira msonkhano. Ndinaona zodabwitsa. Ndege iliyonse yomwe idayima malo omwe ndege yanga ikanaimitsidwa inawonongeka. Ndege yanga, mwachisomo cha Mulungu, sinalipo ndipo motero sinawonongeke. Nkhani yodabwitsa yotsimikizika mokwanira, koma zidachitika bwanji? Ndikutanthauza kuti zinangochitika mwangozi kapena kuti kodi kusakhalapo kwa ndegeyo kunali chifukwa cha lamulo lauzimu lomwe mwanjira ina ndinapezerapo mwayi?

Chabwino, ndikudziwa kuti chinali chotsatira cha lamulo lauzimu limene ndinakhazikitsa, limene ndidzagawana nanu

posachedwapa. Kumvetsetsa lamulo kumakulolani kuti mubwereze zotsatira nthawi iliyonse yomwe mukufuna. Pankhani imeneyi, ndinatsatira lamulo limene Mulungu anandiphunzitsa kalekalelo pamene Mulungu anayamba kundiphunzitsa malamulo ndi zochita za Ufumu Wake.

Ndiloreni ndikusonyezeni lamulo limene Mulungu anandionetsa, ndipo ndidzakusonyezani mmene ndinaligwiritsira ntchito. Kumbukirani kuti nkhani iliyonse ya mu Baibulo imakusonyezani zina zake zokhudza Ufumu ndi mmene umagwirira ntchito. Ndimadzitcha ndekha katswiri wauzimu. Pamene ndimawerenga Baibulo, nthawi zonse ndimayang'ana malamulo amene anayambitsa chinachake kapena malamulo amene sanalole kuti chinachake chichitike. Tikupeza nkhani yomwe ikukhudzana ndi phunziro ili lomwe ndikufuna kukuonetsani mu Maliko 6.

Ndipo pamene dzuwa linapendeka, anadza kwa Iye ophunzira ake nanena, “Malo ano ngachipululu, ndi dzuwa lapendeka ndithu. Muwauze kuti amuke alowe kumilaga ndi midzi yozungulira akadzigulire okha kanthu kakudya.”

Koma iye anayankha nati kwaiwo, “Apateni kudya ndinu.”

Ndipo iwo ananena naye, “Imeneyo ingatenge ndarama yoposa miyezi isanu ndi itatu ya malipiro! Kodi tingapite ife ndikukagula mikate ya pa malupiya a theka mazana awiri ndiko kuapatsa kudya?”

Ndipo Iye ananena nawo kuti, “Muli nayo mikate ingati?” Anafunsa. “Pitani mukaone.”

Ndipo pamene adadziwa ananena, “Isanu—ndi nsomba ziwiri.”

Ndipo anawalamulira kuti anthu akhale pansi onse

mmagulumagulu pa msipu. Ndipo anakhala pansi mabungwe mabungwe a makumi khumi ndi makumi asanu. Ndipo Iye anatenga mikate isanuyo ndi nsomba ziwirizo, nayang'ana kumwamba, nadalitsa, nagawa mikate; napatsa ophunzira kuti apereke kwa iwo. Ndi nsomba ziwiri anagawira onsewo. Ndipo anadya iwo onsewo nakhuta. Ndipo anatola makombo, mitanga khumi ndi iwiri, ndiponso za nsomba. Ndipo amene anadya mikate iwo anali amuna zikwi zisanu.

— Maliko 6:35-44

Iyi ndi nkhani yabwino komanso fanizo la Ufumu wa Mulungu. Mikate isanu ndi nsomba ziwiri kudiyetsa anthu zikwi makumi awiri! Koma inu mumati, “Gary, Baibulo limanena kuti kumeneko kunali amuna zikwi zisanu okha.” Inde likutero, koma ndikhoza kuganiza kuti kunali akazi ndi ana komweko. Chifukwa chake ndikuganiza kuti mwina panali anthu pafupifupi zikwi makumi awiri pamenepo.

Pamene ophunzirawo anafika kwa Yesu ponena za nkhani ya chakudya, Yesu anafuna kuwaphunzitsa kanthu kena ponena za Ufumu kotero iye anawauza kuti, “Muwadyeste.” Chabwino, izo zidawadabwitsa kwambiri. Kodi chakudya choterechi akachipeza kuti? Adayankha pozindikira gwero lokha la zofunukira limene amadziwa—kugwira ntchito! Iwo anati, “Chabwino, izo zingatenge miyezi isanu ndi itatu ya malipiro a munthu!” Kuchokera ku madola awo kwa maola ambiri akuona zowawa ndi kukhetsa thukuta la temberero la dziko lapansi, kungakhale kosatheka kuwadyetsa.

Koma mu Ufumu, malamulo osiyanasiyana okhudza kagwiritsidwe ntchito ka zinthu kamapanga kuti zonse zitheke. Yesu akufuna kuwathandiza kuti aone kupitirira dongosolo la temberero

la dziko lapansi ndikuphunzira kuthekera kwatsopano kuchokera mu Ufumu wa Mulungu. Kenako Yesu anawafunsa kuti aone zimene ali nazo kuti adyetse khamu la anthu. Anapita kukayang'ana kenako ndi kunena kuti apeza mikate isanu ndi nsomba ziwiri koma anadziwa kuti sizikadawathandiza. Kenako Yesu anawapempha mkate ndi nsomba. Atazigwira mmanja mwake, anazipempherera ndi kuzidalitsa. Kenako anazibwezeranso kwa ophunzira Ake kuti agawire khamu la anthu. Inde mukudziwa nkhani yonse; anthu onse zikwi makumi awiri anadya mpaka kukhuta, ndipo anatsala madengu khumi ndi mphambu ziwiri.

Mafunso anga ndi awa: “Ndi chifukwa chiyani Yesu anapempha kuti mkate ndi nsomba zibweretsedwe kwa Iye asanawauze kuti azigawire? Chifukwa chiyani Yesu sanangofunsa ophunzira Ake kuti agawire chakudya akachipeza? Kodi iwo anayeneradi kuona kuti Yesu adalitse izo poyamba?” Yankho lolondola ndi lakuti Yesu anayenera kudalitsa mkate ndi nsomba choyamba. Mwaona, mkate ndi nsomba zinali padziko lapansi pansu pa ulamuliro wa anthu pamene ophunzira Ake anazipeza koyamba. Kumeneko, Yesu analibe ulamuliro pa izo. Koma pamene mkate ndi nsombazo zinaperekedwa kwa Iye mofunitsitsa, Iye anazidalitsa. Mawu akuti *kudalitsa* amatanthauza kuyeretsa kapena kulekanitsa. Tsopano, apa pali lamulo la Ufumu likuwululidwa.

Pamene Yesu anadalitsa mkate ndi nsomba, nsomba ndi mkate zinasintha maufumu.

Kwenikweni, mphamvu ya ulamuliro wa mkate ndi nsomba unasintha. Tsopano Mulungu anali ndi ulamuliro wakuchulukitsira anthu mkate ndi nsomba.

Ngati Yesu sakadatenga mkate ndi nsomba ndi kuzidalitsa, sizikadachuluka.

Timagwiritsa ntchito lamulo lomweli tikamadalitsa chakudya chathu, ngakhale ndikuganiza kuti anthu ambiri sazindikira zomwe akuchita popempherera chakudya chawo. Koma kunena mwachidule, tikamapempherera chakudya chathu, chimasintha maufumu, motero timalola Mulungu kutiteteza ku zinthu zilizonse zoipa zimene tingadye. Ndikufuna kuwonjezera ndemanga pamenepa. Ngati tilolera kupitirizabe kudya zakudya zopanda thanzi ndi kudya zinthu zimene ife tikudziwa kuti ndi zoipa kwa ife, tidzatuta zimene tafesa. Koma tikadya chinthu choopsa, chimene sitizindikira kuti chitivulaza, Mawu a Mulungu atiteteza monga mmene anatetezera ndege yanga. Sindikunena za mtundu wa mapemphero omwe mumamva anthu ambiri akupempherera chakudya chawo. Koma kupemphera ndi chikhulupiriro, kuthokoza Mulungu kuti Iye amachotsa matenda pakati pathu zimatilola, monga nzika za Ufumu Wake waukulu, kusangalala ndi malonjezo Ake.

*Ndipo pamene akumwa kanthu kakufa nako,
sikadzawapweteka.*

— Maliko 16:18

Mdziko lamakonoli, timafunikira chidaliro cha chitetezo cha Mulungu kuti chitipatse mpumulo. Pali zinthu zambiri zimene zingawononge mtendere wathu kumbali zonse, kuphatikizapo chakudya chimene timadya. Mundikhulupirire, mungakhale otsimikiza kuti Satana ali ndi chiwembu chakuba thanzi lanu ndi

luso lanu kuti mukhale motsutsana naye padziko lapansi kudzera mu chakudya!

Tingaone chitsanzo china cha kubweretsa mavuto athu, nkhani, mtendere wathu wa maganizo, kwenikweni chilichonse mmiyoyo yathu pansu pa ulamuliro wa Ufumu pa Afilipi 4:6-7.

Musadere nkhawa konse, komatu mzonse ndi pemphero, ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana chidziwitso chonse, udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Kristu Yesu.

— Afilipi 4:6-7

Tikamapempherera china chake, chimabweretsa vuto kapena nkhani imeneyo mu Ufumu wa Mulungu. Ngati sitipempherera icho, manja a Mulungu amakhala omangidwa. Motero Baibulo limati pempherani kosaleka (1 Atesalonika 5:17) ndipo mulibe chifukwa simupempha Mulungu (Yakobo 4:2).

Pamene ndinagula ndege yanga ndi pamene ndimagula chilichonse, ndimachipempherera, ndikuika manja anga pa icho, kuchibweretsa pansu pa ulamuliro wa Ufumu wa Mulungu kuti chikwaniritse zomwe chidakonzedwera potumikira Ufumu wa Mulungu ndi ntchito yanga. Chifukwa cha ichi, ndege yanga yachoka kwa Satana ndi ziwanda zake. Palibe choipa chidzandigwera mu ndege imeneyo!

Pafupifupi mwezi umodzi wapitawo, ndinali kuuluka m' *Mirage* kuchokera ku Houston kupita ku Ohio titatha msonkhano. Unali usiku pamene tinadutsa mmalo yamdima. Mphezi inaunikira kumwamba chapatali kumanja kwathu ndipo kumanzere kwathu

pamene mphepo yamkuntho inali kuyendanso mdziko lonselo. Mphepo yamkunthoyo inatipangitsa kuti tisinthe njira yathu kuti tipewe chimphepocho, ndipo chifukwa cha izi, tinagwiritsa ntchito mafuta ambiri kuposa momwe tidakonzera. Choncho pofuna kuonetsetsa kuti tikafika kunyumba motetezeka komanso mokwaniritisa malamulo a *FAA* okhudza malo osungira mafuta, tinaganiza zoima ku Louisville, Kentucky, kuti tikagule mafuta. Tinafika tili ndi magaloni makumi atatu, tinali ndi ola limodzi loti tifike ndipo sitinafune kuti tisowe mafuta. Tinafika mu *FBO* ndikuwapempha kuti aike magaloni makumi awiri mu thanki iliyonse yamapiko. Izi zinatitengera mpaka magaloni makumi asanu ndi awiri, yokwanira kuti tiwuluke mtunda wotsalira kupita ku Ohio chifukwa Mirage imagwiritsa ntchito pafupifupi magaloni makumi awiri ndi mphambu ziwiri pa ola.

Pamene tinali kudikirira mu *FBO*, mtsikana wogulitsa anatiuza kuti akhoza kuthira magaloni makumi anayi. Pamene ananena zimenezi, wolozera ndegeyo anabwera ndi mapepala okhudza ntchitoyo. Mtsikanayo anawatenga mmanja mwake, ndikuwayang'ana, kenako ndi kunena kuti, “Pali cholakwika pamenepa. Manambalawa sakufanana.” Wolozerayo anati anaikamo mafuta ndipo atha kukonza manambala patsogolo. Anati, “Chabwino,” koma adati mpaka manambala atakonzedwa, sangandipatse lisiti koma anati adzalitumiza pa *email*. Ife tinati, “Chabwino,” ndipo tinatuluka kupita ku ndege ndi wolozelayo. Woyendetsa ndege wanga anafunsa wolozela ndegeyo kuti atsimikizire ngati anaikadi magaloni makumi awiri mbali iliyonse, ndipo iye anati, “Inde, ndaika magaloni makumi awiri mbali iliyonse.”

Chotero tinanyamuka kupita ku Ohio, ndipo pafupifupi mphindi makumi anayi mu ndege yathu, mwadzidzidzi, thanki

lakumanzere linatha mafuta. Tinadabwa kwambiri; kuti zinachitika bwanji? Patatha mphindi imodzi, thanki yakumanja linathanso mafuta. Panali pakati pausiku kuli mdima, ndipo tinali pamtunda wa ma *feet* zikwi khumi ndi mphambu zisanu opanda kuunika. Chinachitika ndi chiyani? Tidaikamo mafuta. Anthu adzafunsa kuti, “Kodi ndege yanu ilibe zolozera mafuta?” Inde, koma zolozera mafuta za ndege yathu zimakwera pang’onopang’ono pamene pothiramo mafuta. Ngati munayendetsapo *Suburban* yakale,

**PALI MALAMULO
MU UFUMU AMENE
MUYENERA
KUPHUNZIRA KUTI
MUCHITE BWINO,
MUKHALE OTETEZEKA,
NDI KUKHALA NDI
ZOFUNIKIRA PANO
PADZIKO LAPANSI.**

mutha kumvetsetsa zomwe ndikunena. Zolozera mafuta aawo zimakwera pang’onopang’ono pamene mafuta akuwonjezedwa.

Choncho, pamenepa woyendetsa ndege wanga anafunsa wolozerayo ngati anathiradi mafuta okwanira. Ifenso tinamuona ali ndi galimoto yonyamula mafuta akuthira mafuta mu ndege. Woyendetsa ndege wanga mwa khama lake, anaona galimoto yamafuta ikuthira mafuta mu ndege ndikutsi-mikizira kuti magaloni makumi anayi adaikidwa mu ndege. Tikatsimikiza kuti mafuta aikidwa, timaika cholozera mafuta cha *digital* chomwe chimayang’ana momwe mafuta athu atenthedwera ku gawo limodzi la galoni la mafutawo. Tidaganiza kuti tinachita zonse zofunikira ku mbali yathu kuti tiyende bwino.

Tinapempha kutera mwadzidzidzi ku Greater Cincinnati Airport, chinthu chomwe chinalibe vuto popeza tinali pamwamba pake pamene mafuta anatha, zinali zokondweretsa ndithu.

Pofufuza, tinaona kuti inali ndege yake yoyamba imene wolozerayo anathiramo mafuta. Anaika magaloni awiri ku thanki lililonse osati makumi awiri. Samadziwanso kuwerenga mita. Zoonadi? Ndipo ndizo zonse zomwe *company* yadziko imachita ndi ndege zamafuta—zodabwitsa!

Chomwe mdaniyo anali kutanthauza kuti chivulaze sichinali nkhani kwenikweni, koma chikanakhala nkhani yaikulu ngati mafuta akadatha kwina kulikonse koma osati pa ma *feet* zikwi khumi ndi mphambu zisanu. Komanso, mdaniyo sangandivulaze ine kapena ndegeyo. Kuti tigonjetse kuyesa kwina kwa mdani wathu, tinasintha machitidwe pothira mafuta. Tsopano sitisiya wolozera ndege kuti azithira mafuta popanda ife kukhala pomwepo ndi iye tikuyang'anira zonse pothira mafuta. Chochitikacho chikanakhala choopsa kwambiri ngati tikadakhala motsika ndi modekha poyandikira mnthawi yoipa; koma ndithudi, sizinatero monga ine ndili ndi pangano la chitetezo.

Zochitika zonsezi ndi ndege yanga ponena za chitetezero cha ndegeyo pamodzinso ndi ineyo, zinali zotsatira za pangano langa, ufulu wanga wa ulamuliro mu Ufumu. Inde ndikhoza kukuuza nkhani ya momwe ndinapezera ndegeyo poyamba, koma sindidzatero pakali pano. Ndikuganiza kuti mukumvetsa fundoyi—Mulungu ndi wodabwitsa!

Pali malamulo mu Ufumu amene muyenera kuphunzira kuti muchite bwino, mukhale otetezeka, ndi kukhala ndi zofunikira pano padziko lapansi. Satana amatida, koma sangatiletse, atamandike Mulungu. Chitetezo ndiwo mpumulonso, osadandaula, komanso osaopa! Ndi ufulu wanu wa ulamuliro.

Chomwecho, lamulo lomwe ndangofotokoza ndikuligwiritsa ntchito ndilomwe ndimalitcha lamulo la mphamvu yaulamuliro, mwina mukudabwa.

Lembo lina limene Mulungu anandipatsa pachiyambi lonena za Ufumu Wake linali Luka 6:20.

Odala osauka inu, chifukwa uli wanu ufumu wa Mulungu.

— Luka 6:20

Drenda ndi ine tinayamba kuphunzira zimene Mulungu anali kutanthauza ponena za “ufumu wa Mulungu” mu Lembo ili pamene Ambuye anatisonyeza izo koyamba. Apanso, Iye anatisonyeza kuti Iye ndi mfumu ya ufumu, umene umalamuliridwa ndi kugwira ntchito mwa malamulo. Mwachitsanzo, tiyeni tione malire athu akummwera. Chaka chilichonse, anthu zikwizikwi amayesa kulowa mu United States. Chifukwa chiyani? Kodi ndi chifukwa chakuti alibe malo okongola kumene amakhala? Ayi ndithu. Iwo akuyesera kubwera ku United States chifukwa cha boma lakuno. Boma lathu lili ndi malamulo amene amateteza ufulu wa anthu komanso amapereka ufulu wambiri umene kulibe mmaiko ena: kukhala ndi katundu, ufulu wokhala ndi malonda yanu, ufulu wachipembedzo mmene mukufunira, ndi ufulu wolankhula. Zonse sizipezeka mmaiko ena ambiri.

Takambirana kale zambiri za Ufumu wa Mulungu, womwe uli maziko a mafungulo, fundo ndi malamulo onse amene Mulungu watipatsa monga nzika. Kudziwa kwanu kapena kusazindikira kwa malamulowa kungakhale kusiyana pakati pa moyo kapena imfa, chigonjetso kapena kugonjetsedwa. Pambuyo pa kuvutika mzaka zisanu ndi zinayi zimenezo za mantha ofooketsa a zachuma ndipo tsopano kukhala mfulu, sindingathe kutsimikizira mokwanira kufunika kwa kudziwa tanthauzo la kukhala nzika ya Ufumu wa

Mulungu ndi kufunika kwa kudziwa malamulo ndi fundo zonse za makhalidwe abwino zimene zimapanga Ufumu umenewo.

Kwa zaka zikwizikwi dziko lapansi linalipo, komabe zinthu zambiri zimene tikusangalala nazo masiku ano sizinali zomvetsetseka. Mwachitsanzo, ndikufuna kuti muone momwe zinaliri pa Krisimasi usiku mu 1906 ku Ocean Bluff Brant Rock, Massachusetts. China chake chinachitika chimene chinasintha dziko tsiku limenelo. Reginald Fessenden anali kuimba nyimbo ya *Oh Holy Night* ku sitima zapamadzi panyanja kudzera pa wailesi ndipo anali kuwerenga Luka mutu 2. Aka kanali koyamba kuulutsa mawu pa wailesi padziko lonse lapansi. Tsopano, timatenga foni yammanja ndipo timatha kulankhula ndi aliyense padziko lapansi popanda kuganizira.

Kapena bwani za January, 1879? Thomas Edison anakonza koyamba *bulb* lounikira bwino, ndipo tsopano dziko lililonse padziko lapansi limagwiritsa ntchito malamulo a magetsi ndi malamulo amene amalamulira *physics* poonera usiku.

Kapena bwani za December 17, 1903? Pa chichimwene cha a Wright anaulutsa bwinobwino ndege yoyamba, ndipo tsopano tikhoza kukwera ndege yamakono ndi kuwuluka padziko lonse lapansi mu nthawi yochepa chabe. A380, ndege yaikulu kwambiri, yolembera mapaundero 1.2 *million*, imatha kuuluka ndi anthu oposa mazana asanu ndi atatu kwa maola oposa asanu ndi mphambu zinayi popanda kuwonjezera mafuta pa ma mailosi mazana asanu ndi chimodzi pa ola padziko lonse lapansi. Anthu akadaona zinthu ngati zimenezi mzaka za mma 1800, akadakomoka ataona zimenezi. Koma tsopano, sichachilendo kwa ife monga kutembenuza choyatsira magetsi.

Fundo imene ndikunena ndi yakuti malamulo onsewa analipo kale, nthawi zonse anali padziko lapansi, kuyambira kalekale pamene munthu analengedwa. Nthawi zonse zinali zopezeka kuti munthu azizigwiritsa ntchito; koma sanazione basi. Anaona mbalame zikuuluka, anaona mphezi, koma sanamvetsetsebe.

Ndi chimodzimodzinso ndi Malembo. Chipembedzo chaika malire pa zimene Mawu a Mulungu amatanthauza. Inu ndi ine takhala tikumva, kwa zaka zambiri, kuti zonsezo zapita, Mulungu sachitanso zozizwitsa. Mphatso za Mzimu zinali za atumwi okha, kapena munga wa Paulo unali matenda. Kunena zooni, Mawu ndi osavuta. Amatanthauza zenizeni zimene amanena. Koma maziko mu Ufumuwo ndiwo fungulo yaikulu yoyamba imene muyenera kukhala nayo kuti mutsegule zitseko zina zonse.

Tsopano Nayi Fungulo Yina Yaikulu:

Malamulo Sasintha!

Gwetsa thanthwe ndipo lidzagwa. Lidzagwa kangati? Nthawi iliyonse! Lamulo la mphamvu yokokera pansu limatsimikizira kuti mudzalandira yankho lomwelo nthawi zonse. Ndi chimodzimodzinso ndi Ufumu wa Mulungu.

MUTU 5

KUYENDA PA NDEGE NDI KWABWINO KUPOSA KUYENDA NDI MIYENDO

Kuyenda pa ndege ndi kwabwino kuposa kuyenda ndi miyendo! Pamene ndinalembe mutu uwu, ndinali kuuluka kuchokera kunyumba yathu yachilimwe ku Canada mu ndege yangayanga, ndikuyendama mailosi mazana awiri ndi makumi asanu pa ola limodzi ma *feet* zikwi makumi awiri ndi zitatu kuchokera pansu. Kwa zaka zambiri, tinali kupita ku Canada kuchokera kunyumba kwathu ku Ohio. Zimatenga maola makumi atatu ndi mphambu imodzi kuti tifike kumeneko. Ndinali kufunika kuyendetsa galimoto usiku wonse kuti ndikafike tsikulotsatira. Inde, panali nthawi zingapo zomwe timapumula ulendowu popeza unali wa masiku awiri kufika kumeneko, koma mukakhala ndi tchuthi cha milungu iwiri ndipo masiku anayi oyendetsa galimoto, mumataya nthawi yochulukira pameneko. Koma, ya-aa, ndinali wotopa pamene tinafika kumeneko, ndipo ndinayenera kubwerera ndi galimoto yomweyo kuyenda ulendo wa maola makumi atatu ndi mphambu imodzi kubwerera ku Ohio.

Pokhala wokonda ndege ndinapeza *license* yoyendetsa ndege ndili ndi zaka khumi ndi mphambu zisanu ndi zinayi, ngakhale ndinali ndisaganize zokhala ndi ndege. Ndikutanthauza kuti, kodi munaonapo mtengo wandege? Koma pamene ndinali kuphunzira zambiri za Ufumu, ndinazindikira kuti ineyo ndi amene ndinali kuletsa kugula ndegeyo ndi maganizo anga akuti “Ayi” ndiponso maganizo anga aumphawi. Ndili ndi ndege ziwiri tsopano, imodzi yoyamba ndimangoyenda nayo mongosangalala, inayo ndi yomwe ndimagwiritsa ntchito poyendera za ntchito. Monga ndanenera mmutu wapitawu, “Kusaphunzira” kwathu sikulola maloto kapena zothekera. Timawatseka asanayambe.

Ndinali ndisanaganizapo zokhala ndi ndege. Sindinaone mmene zingakhala zotheka. Kwa zaka zambiri, ndinali kuchita *rent* ndege zimene ndinali kukwera. Koma nditayamba kuphunzira za malamulo a Ufumu komanso kuona nkhani zambiri zokhudza Ufumu wa Mulungu pa moyo wanga, ndinaganiza zoti ndikhulupirire kuti Mulungu adzandipatsa ine ndege yangayanga. Panthawiyo ndinalibe ndarama zogulira imodzi, koma ndinatenga cheke, ndipo mu chigawo cha zikumbutso ndinalimba kuti “ndege yanga.” Ndinatchula mtundu weniweni wa ndege yomwe ndinali kulandira. Ine ndi mkazi wanga tinafesa cheke chimenecho cha kulowa Ufumu mogwirizana ndi Maliko 11:24, pokhulupirira kuti ndinalandira pamene ndinapemphera. Izi ndi zimene Yehova anandionetsa poyamba pa nkhani ya Ufumu. Ndinazionapo izi zikuphindula mmoyo wanga nthawi zambiri.

Patapita milungu ingapo, ndinapita kokayesedwa ndipo dokotalayo anangondiiza kuti, “Mwamwayi, kodi mukudziwa aliyense amene angakonde kugula ndege?” Ndinadabwa, popeza palibe amene anandifunsapo zimenezo. “Ndi ndege ya

mtundu wanji?” Ndidafunsa. Anapitiriza kufotokoza zomwe ndegeyo idalili ndipo adandiuza kuti ili pawalo la ndege la komweko ngati ndifuna kuti ndikaone. Modabwitsa, inali yeniyeni ya mtundu wa ndege imene ndinafesera mbewu! Ndinapita pafupi ndi bwalo la ndege ndikuyiyang’ana, ndipo inali yooneka bwino. Ndinadziwa kuti iyi inali ndege yanga. Koma panali vuto limodzi; ndinalibe ndarama zogulira ndegeyo. Ndinauza dokotalayo kuti ndinali ndi chidwi kwambiri ndi ndegeyo ndipo ndidzabwereranso kwa iye.

Patapita milungu ingapo ndinalandira foni kuchokera kwa mchimwene wanga yemwe anali kugwira ntchito ku *restaurant* ya bambo wanga pafupi ndi nyumba yanga ina. Ndinali nditangolandira kumene nyumbayi miyezi ingapo mmbuyomo chakumapeto kwa dzinja. Ndinali ndikukonzekera kusandutsa nyumbayi kukhala maofesi anga a *company* yanga ya zachuma. Nyumbayi sinamangidwe mogwirizana ndi malamulo anyumba yochitira malonda monga ndinali kufunira, motero panafunika kuti ndiimangenso. Ndidalumikizana ndi womanga yemwe adapanga dongosolo lake, ndipo tinasainirana pangano lake. Komabe, tinaganiza kuti tidikire mpaka nyengo ya masika tisanayambe ntchitoyo. Kukonzanso kudzaphatikizapo kumangidwanso kwathunthu kwa nyumbayo.

Mwini wake wakale wa nyumbayo anandiuza kuti madzi anatsokedwa mu nyengo yachisanu, ndipo ndinali ndisadakayang’ane. Mchimwene wanga anandiimbira foni kumapeto kwa February nthawi yotentha itatha pamene *snow* idayamba kusununguka. Anandiuza kuti nyumba yanga yawonongeka chifukwa madzi akutulukira mumsewu. Iye ndi ine tinadziwa tanthauzo la zimenezo—madzi anali asanatsekedwe monga momwe mwini nyumba woyamba ananenera. Ndithudi, pamene ndinayang’ana

zoonongekazo, zinali mapaipi a zimbudzi za mchipinda chapamwamba, pamodzi ndi bafa lapansi ndi mapaipi akukhitchini, zinali zitaphulika ndipo madzi anadzaza mnyumbayo. Mipando yonse, denga, ndi makoma onse anali atagwa kuchokera pazipilala.

Poyamba, izi zinatha kuoneka ngati tsoka lalikulu, koma dongosolo langa lokonzanso lidafuna kuti makoma onse achotsedwe ndikukonza zipinda zatsopano. Mbali yakunjayo inayeneranso kusinthidwa. Choncho kunena zoono, madziwo sanawononge nyumbayo. Zowonongeka zili zonse zomwe zidachitika ndi malo omwe amayenera kumangidwanso. Komabe, nditagula nyumbayo, ndinayiika pa *insurance*. Zowonongekazo zinalipiridwa, ndipo *company* ya *insurance* inandilemba cheke—ndipo muganiza bwino—ndi imene inalipira ndege yanga. Ndege imeneyo, ya *Piper Warrior*, njosavuta kuwulutsa, ndipo ndimayenda nayo kawirikawiri mongosangalala chabe. Nthawi zonse ndikawuluka, ndimadabwa ndi momwe zimakhallira bwino kukwera ndege yomwe idalipiridwa ndarama. Ndikadali nayo ndi ndege imeneyo, ikadayendabe kwa zaka zopitirira makumi awiri.

Ngakhale munkhaniyi zomwe zidachitika zidali zodabwitsa kwambiri, sindikufuna kukusiyani ndi malingaliro olakwika momwe zinthu zimayendera. Zinthu sizimaonekera mwadzidzidzi monga momwe ziliri mu nkhaniyi. Mulungu akhoza kukutsogolerani ku mwayi wopezera ndarama zolipirira ndege yanu, kapena mutha kupeza ndarama zambiri pa nthawi imodzi. Maganizo amene mukufuna kukhala nawo pamene mufesa mu Ufumu ndi akuti Mulungu adzakusonyezani zokolola ndi dongosolo la kulandira. Chinthu chachiwiri ndi kukhala mu chikhulupiriro ndi luso lanu. Ndakhalapo ndi anthu oganiza kuti popeza Mulungu amadzawasonyeza momwe angalipire galimoto yawo kuti apitirize

kubzala \$1 *trillion*. Mulibe chikhulupiriro cha ndarama yokwanira *trillion!* Yambani ndi kugwiritsa ntchito malamulo a Ufumu ndi kukulitsa chidaliro chanu mu malamulo a Ufumu ndi kukhoza kwanu kugwiritsa ntchito zimene Mulungu amakusonyezani.

Koma nayi fundo yomwe ndikufuna kuti muigwire. Ndinakhala woyendetsa ndege kwa zaka zoposa makumi awiri ndisanagule ndegeyo. Kodi mukuganiza kuti malamulo a Ufumu anagwira ntchito zaka makumi awiri mmbuyomo? Ndithudi iwo anatero. Kumvetsetsa kwanga, kapena ndinene kusamvetsetsa kwanga, sikunandilole kuganiza zokhala ndi ndege.

Munthu wakhala akuyang'ana mbalame zikuuluka kwa zaka zambiri, lamulo lonyamula katundu limagwira ntchito masana kuti anthu onse aone, koma palibe amene analiona. Kodi chimene simukuchiona ndi chiyani? Taganizirani izi.

Limodzi la Malembo amene Mulungu anandiphunzitsa mmasiku oyambirira onena za kupuma pa zofunikira za Ufumu linali Miyambo 10:22.

Madalitso a Yehova amabweretsa chuma, ndipo saonjezerapo mavuto.

— Miyambo 10:22

Lembo ili likunena za Mawu ndi fundo zochokera pa Genesis 3:17 zomwe ndidanena kale.

Nthaka ikhale yotembereredwa chifukwa cha iwe; chifukwa cha zowawa udzadyako masiku onse a moyo wako. Idzakuberekera minga ndi mitula, ndipo udzadya zomera zakutchire. Mu thukuta la nkhope yako udzadya chakudya,

*kufikira udzabwerera kunthaka, popeza kuti unatengedwa;
pakuti ndiwe fumbi, ndi kufumbiko udzabwerera.*

— Genesis 3:17-19

Adamu atataya Ufumu, anataya zofunikira za Ufumuwo ndipo anatsala ndi kuyesayesa kwake kuti apulumuke. Koma monga momwe inu ndi ine tadziwira kale, sitingathe kuthamangathanag mokwanira ndi ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta kuti tifike pa ufulu umene timauyembekezera. Koma tsopano pali nkhani yabwino!!!! Yesu anabwera kudzalalikirira uthenga wabwino kwa osauka!

Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine, chifukwa Yehova wandidzoza kuti ndilalikire uthenga wabwino kwa osauka.

— Yesaya 61:1

Yesu anatumidwa kukalalikila uthenga wabwino kwa osauka. Kodi uthenga wabwino ungakhale wotani kwa osauka? Zosavuta, sayenera kumangidwa ndi kusowa ndi umphawi mu dongosolo la temberero la dziko lapansi la zofunikira. Ndikhulupirireni, ndidakhala ndi moyo—kapena ndinene ndinapuluma—kwa zaka zisanu ndi zinayi wopanda chilichonse koma ngongole ndi kupsinjika mmaganizo, Lembo ili linali nkhani yabwino, komabe linali lododometsa. Kodi zidatanthauzadi zimene lidanena? Kodi sizingakhale zabwino ngati linatanthauza kwenikweni zomwe lidanena, kuti dalitso la Ambuye linabweretsadi chuma mmiyoyo yathu? Ndidafunikiradi kudziwa ngati izi zinali zoona komanso momwe ndingagwiritsire ntchito. Komabe, chinthu chimodzi chimene ndinachimvetsa chinali chakuti temberero la ntchito yowawa ndikukhetsa thukuta ndilokhalo lidapereka mlingo wa

kupulumuka—ndipo kupulumuka sikunali kokwanira. Palibe amene anali kufuna kumasuka ku tembereroli kuposa ine, komabe ndinalibe chidziwitso cha momwe ndingakwaniritsire izi mmoyo wanga. Ndikuganiza kuti umu ndi momwe Akristu ambiri amakhalira—kuwerenga malonjezo a Mulungu koma osadziwa momwe angawakwaniritsire ndikuwaonetsera pano mmiyoyo yawo.

Pamene ndinayamba kuphunzira ndi pamene Yehova anandit-sogolera mkumvetsetsa kwanga mu fundo za Ufumu, ndinawerenga mmene Abrahamu analiri wolemera kwambiri. Imani! Nanga bwanji dongosolo la temberero la dziko lapansi; anagonjetsa bwanji zimenezo?

Abramu anali wolemera kwambiri pa ziweto ndi siliva ndi golidi.

— Genesis 13:2

Anakhala wolemera—ayi, Baibulo limati anali wolemera kwambiri—koma motani? “Chabwino,” mwina munganene, “zinali chifukwa chakuti iye anali Abrahamu.” Ayi, sizinali choncho, ndipo apa ndipamene muyenera kumvetsetsa za Ufumu wanu. Malamulo salabadira kuti ndinu ndani alibe tsankho pa munthu. Ngati wina, aliyense, adalumpha kuchokera ku Empire State Building popanda parachuti, mosasamala kanthu kuti anali wamkulu kapena wamng’ono bwanji, aliyense angadziwe zotsatira zake. Lamulo la mphamvu yokokerapansi lidzagwira ntchito nthawi zonse. Ndiye kodi Abrahamu anapambana bwanji ngakhale kuti dziko lapansi linali ndi temberero? Kodi mu nkhani yake muli malangizo amene tingapeze? Gawo la yankho likupezeka mu Genesis 12. Pamenepo, Mulungu anapatsa Abramu, pambuyo pake kuti akhale Abrahamu, lonjezo lokhudza moyo wake ndi mbadwa zake.

Yehova anati kwa Abramu, “Tuluka m’dziko lako, ndi kwa abale ako ndi ku nyumba kwa atate wako, kunka ku dziko limene ndidzakusonyeza iwe. Ndipo ndidzakuyesa iwe mtundu waukulu, ndipo ndidzakudalitsa iwe; ndikubukitsa dzina lanu, nukhala iwe dalitso; ndipo ndidzadalitsa amene akudalitsa iwe, ndikutemberera iye amene akutemberera iwe; ndipo mwa iwe adzadalitsidwa mabanja onse a dziko lapansi.”

— Genesis 12:1-3

Lonjezolo linali lodalira pa Abrahamu kukhulupirira Mulungu ndi kumvera Iye, ndipo zinatengera chikhulupiriro chachikulu kutuluka osadziwa kumene akumukako.

Ndi chikhulupiriro Abrahamu, poitanidwa anamvera kutuluka ku malo amene adzalandira ngati cholowa, ndipo adatuluka osadziwa kumene akumukako.

— Aheberi 11:8

Chotero tikupeza kuti Mulungu anapeza mwalamulo njira yolowera mmalo a dziko lapansi kupyolera mwa munthu amene anamkhulupirira ngakhale pamene zinali zosamveka. Chikhulupiriro cha Abrahamu chinapangitsa Mulungu kumdalitsa iye mwini. Koma pambuyo pake, chifukwa cha chikhulupiriro cha Abrahamu, Mulungu anapanganso naye pangano lokhudza olandila cholowa chake. Musaganize kuti izi ndi zachilendo. Kumbukirani, umu ndimo mmene Satana mwiniyo analowera m’dziko lapansi pachiyambi. Adamu, amene anali ndi mphamvu yaulamuliro padziko lapansi, monga momwe kwalembedwera pa Aheberi 2:7-8, anasankha kukhulupirira Satana mmalo mwa Mulungu.

Chikhulupiro cha Abrahamu, chimene chinatsegula khomo lalamulo la chisonkhezere chakumwamba mmoyo wake, chinamulola kuchita bwino kwambiri. Kulemera kumeneku kunafalikira kupyolera mu olandila cholowa cha Abrahamu. Pamene ndinapitiriza kuphunzira zimenezi, ndinapitiriza kuwerenga za Yosefe, mdzukulumtengo wa Abrahamu. Ndinapeza fanizo lalikulu ndi kumvetsetsa kwa Ufumuwo ndi mmene umagwirira ntchito, ndipo makamaka, zimene Miyambo 10:22 imatanthauza.

Kuti athetse vutoli, abale ake a Yosefe anamuda ndipo anamugulitsa mu ukapolo kudzera mwa anthu ochita malonda ya ukapolo amene anali kuyenda kawirikawiri mdera lawo. Iwo anatenga Yosefe ndi kupita naye ku Aiguputo, kumene anakagulitsidwa kwa Potifara, mkulu wa asilikali a ku Aiguputo. Munali mu mawu otsatirawa pomwe ndidapeza gawo lalikulu pamalingaliro okhudzana ndi kuthekera kwa Abrahamu kuchita bwino momwe adachitira.

Ndipo anatsika naye Yosefe kunka ku Aigupto. Ndipo Potifala, nduna ya Farao, kazembe wa alonda, M-aigupto anamugula iye mmanja mwa Aismayeli amene anatsika naye kunka kumeneko. Yehova anali ndi Yosefe ndipo iye anali wolemeralemera, nakhala mnyumba ya mbuyewake M-aigupto. Ndipo mbuyewake anaona kuti Yehova anali ndi iye, ndi kuti Yehova adamlemereza mdzanja lake zonse anazichita, Yosefe anapeza ufulu pamaso pake ndipo anamtumikira iye.

Potifala anamuyesa iye woyanganira panyumba yake, naika mmanja mwake zonse anali nazo. Ndipo panali chiyambire anamuyesa iye woyang'anira pa nyumba yake ndi pa zake zonse, Yehova anadalitsa nyumba ya M-aigupto

chifukwa cha Yosefe. MDALITSO WA YEHOVA UNALI PA ZAKE ZONSE, MNYUMBA NDI MMUNDA. Ndipo iye anasiya zake zonse; mmanja mwa Yosefe, osadziwa chomwe anali nacho koma chakudya chimene anadya.

— Genesis 39:1-6

Lemboli limanena momveka bwino kuti ndi madalitso a Yehova amene anachititsa kuti Yosefe akhale wolemvera. Koma kodi Dalitso la Ambuye linali chiyani kapena ndi chiyani? Ine ndinazindikira kuti awa anali “Madalitso” a Ambuye, osati “mdalitso” wa Ambuye. Tonsefe ponena za chinthu chachikulu titha kuti “linali dalitso.” Koma lemboli silikunena za chinthu chabwino chomwe chikuchitika. Lilikunena za “Madalitso.”

Ndinazindikira kuti Madalitso a Yehova anali pangano limene Mulungu anapanga ndi Abrahamu ndi olandira cholowa chake. Kwenikweni Madalitso anali malonjezano operekedwa kwa Abrahamu mpangano limenelo. Pangano lalamulo lili ndi ntchito ndi udindo wa onse okhudzidwa, koma limafotokozanso ubwino wa aliyense. Pamenepa, malonjezano operekedwa kwa Abrahamu anali mbali ya phindu la panganolo. Udindo, kuti tisangalale ndi maphindu amenewa, unali kutsatira malangizo ndi malamulo a Yehova. Ndidaonanso momveka bwino kuti chilichonse chomwe Yosefe adabweretsa pansi paulamuliro wake mwalamulo chinalinso pansi kapena kusangalala ndi malonjezo kapena maphindu omwewo.

Tsono Miyambo 10:22 linali lomveka kwa ine. Malonjezo a Mulungu operekedwa kwa Abrahamu monga pangano lalamulo anathetsa dongosolo la temberero la pdziko lapansi la umphawi. Madalitso operekedwa kwa Abrahamu anapangitsa kukhala

kovomerezeka kwa Mulungu kudalitsa Abrahamu ndi mbadwa zake kukutukuka ndi chisonkhezere chimene Mulungu anali kufuna kuti munthu akhale nacho. Tiyeni tsopano tiwerenge Miyambo 10:22 ndi kumvetsa kwathu kolembedwa mu ma *brackets*.

Fungulo Yaikulu:

Madalitso a Yehova [Malonjezo Operekedwa kwa Abrahamu] Amabweretsa Chuma, ndipo Saonjezerapo Mavuto.

Mawu akuti “*saonjezerapo mavuto*” akunena za dongosolo temberero la dziko lapansi lotchulidwa pa Genesis 3:17—kudzera mu ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta. Mawu aChiheberi otanthauza *mavuto* amatanthauzanso ntchito yolemetsa! Kodi inu mukuziona izi? Munthu atha kuthawa temberero la dziko lapansi la ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta kudzera mmalonjezo operekedwa kwa Abrahamu. O-oo, ndikudziwa zomwe mukuganiza—“Malonjezano amenewo anaperekedwa kwa Abrahamu ndi mbewu yake yokha.” Inde, koma ndikufuna ndikuonetseni Lembo lina, Agalatiya 3:13-14.

Kristu anatiwombola ku temberero la chilamulo atakhala temberero mmalo mwathu, pakuti kwalembedwa: “Wotembereredwa aliyense wopachikidwa pamtengo.” Kuti dalitso [malonjezo] la Abrahamu mwa Kristu lichitike kwa amitundu, kuti tikalandire lonjezo la Mzimu mwa chikhulupiro.

— Agalatiya 3:13-14

Tsopano kudzera mchikhulupiriro, ife monga okhulupirira mwa Yesu Kristu timatenga nawo mbali mdalitso loperekedwa kwa Abrahamu. Ndilo dalitso lotani kwa Abrahamu? Tingapeze mndandanda wa malonjezo olembedwa mu Deuteronomo 28.

Ndipo kudzali mukamvera mawu a Yehova Mulungu wanu mwa changu, ndi kusamalira kuchita malamulo ake onse amene ndikuuzani lero, kuti Yehova Mulungu wanu adzakukulitsani kuposa amitundu onse pa dziko lapansi. Ndi madalitso awa adzakugwerani, ndi kukukwezani, mukadzamvera Mawu a Yehova Mulungu wanu:

Mudzakhala odala mmudzi ndi odala kubwalo. Zidzakhala zodala zipatso za thupi lanu, ndi zipatso za nthaka yanu, ndi zipatso za zoweta zanu—zoswana za ng'ombe zanu ndi zoswana za nkhosa zanu.

Zodzakhala zodala mtanga wanu ndi choumbiramo mkate wanu.

Mudzakhala odala polowa inu, ndipo mudzakhala odala potuluka inu.

Yehova adzakantha adani anu akukuukirani. Adzakudzerani mnjira imodzi, koma adzathawa pamaso panu mnjira zisanu ndi ziwiri.

Yehova adzakulamulirani dalitso mu nkhekwe anu, ndi mu zonse mutulutsirako dzanja lanu. Ndipo adzakudalitsani mdziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani.

Yehova adzakukhazikitsani inu yekha mtundu wa anthu opatulika, monga anakulumbilirani, ngati mudzasunga malamulo a Yehova Mulungu wanu, ndi kuyenda mu njira zake. Ndipo anthu onse a padziko lapansi adzaona kuti akutchulani dzina la Yehova, nadzakuopani. Ndipo

Yehova adzakuchulukitsirani zokoma—mzipatso za thupi lanu, ndi mzipatso za zoweta zanu ndi mzipatso za nthaka yanu—m'dziko limene Yehova analumbilira makolo anu kuti adzakupatsani.

Yehova adzatssegula kumwamba, nkhokwe Yake ya ubwino, kugwetsa mvula pa dziko lanu mnyengo yake ndi kudalitsa ntchito zonse za manja anu. Mudzakongoletsa kwa amitundu ambiri osakongola nokha. Yehova adzakuyesani mutu, si mchira ayi. Ngati mudzamvera malamulo a Yehova Mulungu wanu amene ndikuuzani lero ndi kuwasunga ndi kuwatsata, nthawi zonse mudzakhala wa pamwamba, osati wapansi. Osapatukira mawu ali onse ndikuuzani lero, ku lakumanja kapena lakumanzere, kutsata milungu ina kuitumikira.

— Deuteronomo 28:1-14

Malonjezano onsewa, ngakhale ali mu Chipangano Chakale, tsopano ndi anu kuti musangalale nawo. Chosiyana ndi chakuti mu Chipangano Chakale anthu anali kuwapeza kudzera mu zimene anachita, koma timawapeza kudzera mu chikhulupiriro chathu mwa Yesu Kristu pansu pa pangano latsopano. Inu ndi ine, monga amitundu, tinalumikizidwa; ndipo tsopano, kudzera mwa Yesu Kristu, ife tigawana mu dalitso la Abrahamu. Koma tili ndi zambiri kuposa madalitso akuthupi a Abrahamu, tili ndi dalitso lauzimu la kubadwa mwatsopano. Ife tsopano tiri mwa kuthupi, ndi mdalitso wapadziko lapansi wa Abrahamu, koma tirinso ndi mdalitso kwenikweni wamuyaya wa kumwamba ndi Mzimu Woyera akukhala mwa ife monga ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Kumbukirani, ana aamuna ndi aakazi okha ndiwo amalandira cholowa; akapolo sangathe. Popanda kubadwa mwatsopano, ngakhale Abrahamu anakonda Mulungu, ngati Mzimu Woyera sadakhala mwa iye,

ndipo sadakatha kulowa kumwamba. Ndithudi, iye analandira kumwamba Yesu atabweza ngongole ya uchimo.

Tsopano ndinamvetsa tanthauzo la Miyambo 10:22 pamene limanena kuti Mulungu ndiye amabweretsa chuma ndipo Saonjezerapo mavuto. *Mavuto* mu chilankhulo cha Chiheberi akutanthauza ntchito yowawa, yomwe ndidamvetsa tsopano kuti ikulozera ku dongosolo la temberero la dziko lapansi la ntchito yowawa ndiyokhetsa thukuta. Ndinamvetsetsa kuti panganoli, dalitso ili la lonjezo la chithandizo cha Mulungu ndi maphindu Ake, linakweza Abrahamu pamwamba pa temberero la dziko lapansi ndi kumupangitsa kukhala wolemera. Ndinazindikira kuti maphindu a dalitso limenelo monga tafotokozera mu Deuteronomo 28, adandi-onetsa momveka bwino kuti ndiyenera kuchita bwino. Zotsatira za malonjezowa zikanakhala kuti ndinapangidwira kukhala mutu osati mchira, wobwereketsa osati wobwereka. Uwu ndi ufulu wovomerezeka wa mwana aliyense wa Mulungu. Monga Yosefe, ine ndiri ndi madalitso a Mulungu, ndipo ine ndiyenera kuchita bwino. Ndilinso ndi cholowa cha Ufumu wonse wa Mulungu. Monga mwana, zonsezo ndi zanga kale mwalamulo.

Pamene ndinayang'ananso nkhani ya Yosefe mu Genesis 39, ndinaona bwino lomwe kuti kupambana kwa Yosefe ndiko kumene kunakopa chidwi cha Potifara, ndipo kunalinso kupambana koonekera kumene kunali kukopa chidwi cha amitundu a dziko ndi kuwalola kuona kusiyana mwa anthu a Mulungu.

Ndipo anthu onse a padziko lapansi adzaona kuti akutchulani dzina la Yehova, nadzakuopani. Ndipo Yehova adzakuchulukitsirani zokoma—mzipatso za thupi lanu, ndi mzipatso

*za zoweta zanu ndi mzipatso za nthaka yanu—m'dziko limene
Yehova analumbilira makolo anu kuti adzakupatsani.*

— Deuteronomo 28:10-11

Panalonso chidziwitso china chachikulu mu Genesis 39:6 chomwe ndidachionanso ndipo ndikufuna kuti muone. Ponena za Potifara, chimati: “*Ndipo iye anasiya zake zonse; mmanja mwa Yosefe, osadziwa chomwe anali nacho koma chakudya chimene anadya.*” Ndinazona! Nachi chitsanzo cha zina zonse zimene tikukamba. Potifara sanali kudera nkhawa pa chilichonse kupatulapo chakudya chimene anali kudya. Izi zikusonyeza kuti chipambano chimene Yosefe anabweretsa pa banja lake, Madalitso a Yehova, chinabala chochulukapo zimene zinalola Potifara kuika maganizo ake pa ntchito yake osati kupulumuka!

Ine ndi Drenda tili ndi mwambi womwe takhala tikugwiritsa ntchito kwa zaka zambiri, “Pokhapokha mutakonza zinthu zandarama, simudzazindikira tsogolo lanu,” ndipo sindidzazindikira kuti ndinu ndani. Simudzapeza mtendere wanu, malo anu owakonda, osakhutitsidwa konse. Mudzakhala mukupanga zitsimikizo zanu zonse zokhudzana ndi kupulumuka, kupeza kapena kusunga ndarama, kukhala munthu wongotulutsa ndarama. Apa tikuona zotsatira za dalitso la Yehova pa Potifara, yemwe sanali kudziwa komwe za Ufumu wa Mulungu. Mwa kuika katundu wake mmanja mwa Yosefe, chuma chake, nkhawa zake zinasamutsidwira pansu pa pangano limene Yosefe anasenza. Mutha kuona bwino nthawi yomwe kusamutsaku kudachitika mu ndime 5 ya mutu 39.

Ndipo panali chiyambire anamuyesa iye woyang'anira pa nyumba yake ndi pa zake zonse, Yehova anadalitsa nyumba ya M-aigupto chifukwa cha Yosefe. Madalitso wa yehova unali pa zake zonse, mnyumba ndi mmunda.

— Genesis 39:5

Pansonso tikuona kusamutsidwa kwa china chake m'dziko lapansi, chimene chili pansi pa dongosolo la temberero la dziko lapansi, kubwera pansi pa ulamuliro wa Ufumu wa Mulungu ndi kusintha kwakukulu kukuchitika. Tinene kuti: Ngati Mulungu akukuthandizani ndi nzeru Zake, kukutsogolerani ku zitsimikizo zolondola, ndi kukuchenjezani za mbuna zomwe mungagweremo, aliyense akhoza kuchita bwino! Kodi inu mukuziona izi? Madalitso a Yehova ndi anu!

Pamene ndinali kuphunzira zimenezi pamene Ambuye anali kundiphunzitsa za Ufumu, ndinasokonezeka chifukwa chimene Yosefe anapambanira kwambiri chinali cha dalitso limeneli, komabe Akristu ambiri amene ndikuwadziwa masiku ano akuvutika kuti alipire ngongole. Kukhala mfulu kwathunthu pazachuma ndichinthu chomwe ambiri sachiganizirapo. Komabe, tili ndi pangano labwino kwambiri lozikidwa pa malonjezano abwino kuposa a Chipangano Chakale. Ngakhale kuti ndinamvetsa bwino za Madalitso a Yehova, sindinadziwebe mmene dalitso limaperekera mayankho amene ndinali kufunikira—koma ndinali kuphunzira ndi kusangalala ndi ufulu wochuluka pamene ndinayamba kugwiritsa ntchito ndi kuyesa zomwe Mulungu anali kundiphunzitsa.

Kenako ndinatembenukira ku Chipangano Chatsopano ndikuyang'ana pa Yesu ndi utumiki Wake kuti ndiphunzire zambiri za mmene Ufumu wa Mulungu unali kusinthira makhalidwe ndi chikhalidwe kumeneko.

Ndipo panali pakumukanikiza khamu la anthu kudzamva Mawu a Mulungu, iye anali kuimirira mmbali mwa ya Genesarete, ndipo anaona ngalawa ziwiri zinakhala mbali mwa Nyanja, koma asodzi ansomba anatuluka mmenemo, nali kutsuka makoka awo. Ndipo iye analowa mngalawa imodzi, ndiyo yake ya Simoni, nampemba iye akankhe pang'ono. Ndipo anakhala pansi mmenemo, naphunzitsa mngalawa makamu a anthu.

Ndipo pamene Iye analeka kulankhula, anati kwa Simoni, “kankhirani kwakuya nimuponye makoka anu kokasodza.” Ndipo Simoni anayankha, nati, “Ambuye, tinagwiritsa ntchito usiku wonse osakola kanthu. Koma pa mawu Anu, ndidzaponya makoka.”

Ndipo pamene anachita ichi, anazinga unyinji waukulu wa nsomba ndipo makoka awo anali kung'ambika. Ndipo anakodola anzawo a mngalawa inayo adze awathangate, ndipo anadza nadzadza ngalawa zonse ziwiri motero kuti zinali nkumira.

Koma Simoni Petro pamene anaona, anagwada pa mabondo ake a Yesu nanena, “Muchoke kwa ine, Ambuye; chifukwa ndine munthu wochimwa!” Pakuti chizizwo chidagwira iye ndi onse amene anali naye pa kusodzako kwa nsomba zimene anazikola, ndipo chimodzimodzinso Yakobo ndi Yohane, ana a Zebedayo, amene anali anzake a Simoni.

Ndipo Yesu anati kwa Simoni, “Usaope; kuyambira tsopano udzakhala musodzi wa anthu.” Ndipo mmene iwo anakocheza ngalawa zawo pantunda, anasiya zonse namtsata Iye.

— Luka 5:1-11

Nayi nkhani ya mmene Ufumu wa Mulungu unasinthira

dongosolo la temberero la dziko lapansi mmiyoyo ya asodzi atatu mmawa wina. Mukawerenga lemboli, mupeza kuti Petro, Yakobo, ndi Yohane anali kusodza usiku wonse osagwira kalikonse. Chitsanzo cha dziko lapansi cha dongosolo la temberero la ntchito zowawa ndizokhetsa thukuta, iwo anasodza usiku wonse osagwira kanthu kusonyeza ntchito yawo. Koma pamene Yesu alowa mu Ufumu wa Mulungu ndi ntchito yake, asodzi amodzimidziwo anakugwira nsomba zambiri kwakuti ngalawa zawo zinatsala pang'ono kumira ndi kulemera kwa nsomba!

Imani!!!! Taganizirani zimene tangowerenga kumene. Palibe, palibe nsomba, panalibiretu, zinasandulika zokolola zomwe pafupifupi zinafunu kumiza ngalawa ziwiri? Komabe anthu amawerenga nkhaniyi ndipo awerenga nkhaniyi kwa zaka mazana ambiri ndipo sakuona kapena kuganiza kuti izi zingachitikebe kwa iwo. Chifukwa cha chiyani? Yankho lanthawi zonse lingakhale lakuti Yesu analipo ndipo anachita. Kumbukirani nkhani yomwe ndidakuonetsani pa Maliko 6 pamene Yesu sakanachiritsa anthu chifukwa anthu analibe chikhulupiriro, motero, Ufumuwo ulibe mphamvu ya ulamuliro? Winawake anayenera kupereka mphamvu ya ulamuliro wakumwamba kumwamba kusanayankhe.

Ndipo Simoni anayankha nati, “Ambuye, tinagwiritsa ntchito usiku wonse osakola kanthu. Koma pa mawu Anu, ndidzaponya makoka.”

Petro adagwirizana ndi kumwamba, ndipo kumwamba kunali ndi mwayi wovomereza mu nkhaniyi. Apanso, tikuona dziko lapansi likusinthidwa ndi Ufumu wa Mulungu. Sizopenga, monga momwe anthu amaonera mbalame zikuuluka kwa zaka zikwi zambiri koma

osazindikira kuti kuuluka ndikotheka kwaiwo kunali kosatsatidwa konse. Ndi chimodzimodzinso ndi Akristu lero lino, sadziwa kuti sayenera kukhala ndi makoka opanda kanthu koma ali ndi mwayi wopeza mphamvu yakumwamba yowathandiza kuchita bwino mu umoyo. Chinthu chomwe ndikufuna kuti muone apa ndichakuti anyamata omwewo amene sanagwire kanthu ndi omwewo ali ndi ngalawa ziwiri zodzadza ndi nsomba zikufuna kumira!

Mnzanga, kusiyana kwake ndi kumeneku ndi Ufumu, osati ndi anthu. Mutha kuganiza kuti mulibe tsogolo, osakwanira, opanda chilichonse chikuyenda bwino. Koma zoonza zake ndi zakuti, zimene mukufunikira ndi Ufumu kuti usinthe moyo wanu kukhala nkhani yopambana. Inde, muli ndi gawo lanu loti muchite. Anayenera kupita kokapha nsomba—anyenera kusamalira makoka awo, ndi kukonzekera kusodza—koma aliyense akhoza kugwira nsomba ngati Mulungu akusonyezani kumene zili.

Mvetserani, dongosolo la temberero la dziko lapansi la kuthaman-gathamanga ndikukhetsa thukuta silingathe kugwira ntchito. Simungathe kuthamanga kokwanira kapena kuthamnaga kotalika mokwanira kuti mukwaniritse maloto anu. Mulungu sanafuna kuti muzikukuta mano ndi kumayesetsa kuchita zinthu ndi mphamvu zanu zokha.

Mwa kulowerera mmalamulo ndi mmalonjezo a Ufumu wa Mulungu, tingaende pandege mmalo moyenda ndi miyendo. Ndiloreni ndiike nkhanayi mwanjira ina. Ngakhale kuti lamulo la mphamvu yokokera pansu likugwirabe ntchito, tingathe kuuluka mwa kulowa mu lamulo lina, lamulo la kukweza zinthu, ndi kusan-galala ndi moyo watsopano.

Kumbukirani, pamene mubwera kwa Kristu, ndinu chiwalo cha wa Ufumu wa Mulungu. Monga nzika, mukupereka ufulu wa ulamuliro; ndipo monga mwana wamwamuna kapena wamkazi,

mukunena kuti muli ndi ufulu wolandira cholowa. Ufulu wanu wa ulamuliro ndi zopindulitsa zakukwezani pamwamba pa dongosolo la temberero la padziko lapansi la umphawi, matenda, ndi kulephera.

Tangoganizirani mmene ndime imeneyi inamvekera kwa M'israyeli amene anakhala kapolo kwa moyo wake wonse. Ndipotu, zimene anali kudziwa zinali ukapolo kuyambira kalekale. Awa ndi mawu amene Mose analankhula kwa mtundu wa Aisrayeli pamene anali kupita ku dziko lolonjzedwa.

Ndipo kudzakhala Yehova Mulungu wanu adzakulowetsani m'dziko limene analumbirira makolo anu, Abrahamu, Isake ndi Yakobo, kuti adzakupatsani ili—midzi yaikulu, ndi yokoma imene SIMUNAIMANGA, ndi nyumba zodzala nazo zokoma zilizonse zimene simunazidzaza, ndi zitsime zosema zimene simunazisema, minda ya mpesa ndi minda ya azitona zimene simunaziwoka—ndipo mutadya ndi kukhuta, pamenepo mudzichenjerere mungaiwale Yehova, amene anakutulutsani m'dziko la Aiguputo [ufumu wina] m'yumba ya UKAPOLO [ufumu waukapolo].

— Deuteronomo 6:10-12

Monga akapolo omwe kale anali mu ukapolo, njira yokhayo imene iwo anadziwira kuti achitepo kanthu inali ntchito yowawa ndiyokhetsa thukuta. Koma apa Mulungu anali kuwauza kuti ntchito yawo siidzawapezera zofunikira. Iye sanali kuwauza kuti sadzagwiranso ntchito iliyonse, koma kuti iwo sadzakhala omangidwa ku dongosolo limene limafuna kugwira ntchito kuti apulumuke. Mulungu akunena kuti zinthu zidzayenda bwino m'dziko limene anali kuwatsogolera.

Ndiloreni nditseke mutuwu ndi nkhani ina yomwe ikuonetseranso zomwe ndikunena. Ine ndi Drenda sitili mu zamagalimoto. Ena anthu ali, ndipo akhoza kukuuzani za magalimoto onse omwe amawasirira. Pazifukwa zina, sitinalowe mu zamagalimoto. Tsopano, musandimwe molakwa. Timakonda zinthu zabwino, koma sitinanenepo kuti tiyenera kukhala ndi galimoto inayake. Nthawi zambiri timagula galimoto kenako kuiyendetsa kwa zaka khumi kapena kuposerapo. Inde, timasamalira bwino magalimoto athu ndipo samaoneka ngati magalimoto akale, koma pokhapokha akamaoneka bwino komanso kuyenda bwino, timasangalala.

Koma zaka zingapo zapitazo, tchalitchi chathu chidachita *rent* ma *Escalade* angapo pamsonkhano womwe tinali kuchititsa. Tinawabwerekka kuti tiziyendetsa alendo athu kuzungulira apo ndi apo, ndipo tinali kufuna kupereka galimoto yabwino kuti ichite ntchito imeneyo. Tsopano, aka sikanali

koyamba kuti tichite zimenezo. Takhala tikuchita zimenezo nthawi zonse. Koma aka kanali koyamba kuti tiyendetse mmodzi wa iwo amene tinali nawo pamalopo ndipo zinachitika. Sindikudziwa chifukwa chake chimene tidayendetsera imodzi panthawiyi, koma tidaiyendetsa kunyumba usiku wina. Ndipo mukudziwa chiyani? Tinaikonda. Ine ndi Drenda tinali kukonda momwe imayendera komanso momwe imaonekera.

Panthawiyoyi, tinali kuyendera *Honda Pilot* yabwino, koma *Escalade* inali ya pamwamba. Inali ya ngale yoyera ndipo inali yaifupi. Ngati mumadziwa zambiri za ma *Escalade* awa, amabwera pawiri, yaitali komanso yaifupi. Tinali kukonda yaifupiyo momwe inali

**ZIMENE
MUKUFUNIKIRA NDI
UFUMU KUTI USINTHE
MOYO WANU KUKHALA
NKHANI YOPAMBANA.**

kuonekera ndipo imayenda bwino, inali yosungika bwino. Pamene ndimayendetsa *Escalade* ndi Drenda anati, “Mukudziwa, ndimakonda iyi; ndikuganiza kuti tipeze imodzi mwa izi.” Ndinavomera. “Tiyenera kupeza imodzi ngati iyi, mtundu waufupi wa ngale yoyera.” Tonse tinavomera.

Ngakhale kuti sitinauze aliyense za kukambirana kwathu, patapita pafupifupi mwezi umodzi, ndikuyenda panja kukatenga pepala langa, foni yanga ya mmanja inalira. Ndinazindikira kuti mawu a mbali ina anali a munthu amene amapita kutchalitchi changa. Iye anati, “Moni,” ndipo ananena kuti akufuna kundigulira *Escalade*. Ndinadabwa kwa mphindi imodzi koma ndinati, “Chabwino!” Kenako anandifunsa mtundu umene ndikufuna, ndipo ndinamuza kuti timakonda ya ngale yoyera. Iye anati, “Ndidzakuuzani ndikadzakupezerani imodzi.” Komabe, sanandifunse ngati ndinali kufuna yaifupi kapena yaitali. Mwezi unatha ndipo ndimaganiza kuti mwina waiwala zagalimoto, koma zoonza, adaimba foni ndikutiuza kuti tipite, watikonzera *Escalade* kuti tikaitenge.

Pamene tinakumana naye, tinaona yokongola ya ngale yoyera, *Escalade* yaifupi ili pamenepo. Inali yabwino mwanjira iliyonse, yopanda zokalika, inali ndi ungiro weniweni. Tinamuza kuti tiikonda. Kenako anapepesa kuti zinatenga nthawi yaitali akuyesa kupeza yaitali, koma adatha kupeza yaifupi. Tinaseka ndikunena kuti, “Yaifupiyo ndi imene tinali kufuna.” Tinayendetsa galimotoyo kupita kunyumba ndipo tinaganiza kuti ndife anthu olemera kwambiri padziko lonse lapansi poyendetsa galimotoyo. Koma mukudziwa chiyani? Ma *Escalade* amenewo akhalapo kwa nthawi yaitali. Sindinaganizepo zakukhala ndi imodzi! Kuti mumvetse bwino nkhanayi, muyenera kudziwa kuti ndapereka magalimoto

asanu ndi atatu mmbuyomo, choncho ndinali nditafesa mbewu pansu ponena za magalimoto. Sindinanene kuti ndikuifuna.

P.S. – Ndikudziwa zomwe mukuganiza, kuti zinthu zamtunduwu zimangochitika kwa alaliki. Eya, ndakhala ndikuchita zandarama kwa zaka makumi atatu mphambu zisanu ndi chimodzi ndipo ndalankhula ndi alaliki ambiri. Kunena zoono, ambiri a iwo sapeza ndarama zambiri. Ayi, zinthu zimenezi sizichitika ndipo sizichitika kwa ife chifukwa cholalikira za Ufumu, koma chifukwa chakuti tikukhala mu Ufumu ndi kugwiritsa ntchito malamulo a Ufumu pa moyo wathu. Ndipotu, ndinali ndi ngongole ndisanayambe tchalitchi changa. Sindinafunikire kuyambitsa tchalitchi changa kuti ndipeze ntchito yolipira ngongole zanga, ndikungonena.

MUTU 6

PALI ZAMBIRI PA UMOYO KOPOSA KUNGOLIPIRA NGONGOLE

Zinali kuoneka ngati malo opumulira kwa kanthawi kochepa kuzovuta za moyo zomwe ndimakumana nazo. Tinaitana anthu pafupifupi makumi asanu ku kanyumba kwathu kakale ka pafamu kukasangalala powotha moto, kunali ma *hot dog* komanso kucheza. Izi zinali mzaka za kupsinjika kwakukulu popanda ndarama, ndikungovutikira kuti ndipulumuke sabata imodzi. Ndinali kuyang'anira kuchochitikacho chifukwa ndinali wotopa mmaganizo ndipo ndinali kufuna china chake chabwino kuti ndiganizirepo pang'ono. Kucheza kunayenda bwino kwambiri: chakudya chinali chabwino, anzathu ambiri anabwera ndi ana awo, ndipo onse anali kusangalala. Mnyumba munadzaza anthu ndipo kenaka pachitseko panamveka kugogoda. Ndidaganiza kuti mwina ndi wina wobwera mochedwa ku msonkhano wathu, koma nditatsegula chitseko, ndidalandiridwa ndi wantchito wa *pacompany* yamagetsi. Adandiuza mwaulemu kuti anabwera kudzazimitsa magetsi chifukwa cha ngongole

yosalipiridwa. Ndinachita mantha. Nyumba yanga inali yodzaza ndi alendo ndipo magetsi amafunika, komanso chinali chinthu cha manyazi kuzimitsa magetsi alendo ali pomwepo.

Mwamsanga ndinapempha wogwira ntchitoyo kuti apite kuseri kwa nyumba kwa mphindi imodzi. Ndinamufunsa kuti ndi ndarama zingati kuti magetsi ayakebe ndipo adandiuza ndarama zake. “Zochulukwa kwambiri,” ndinaganiza. “Kodi mungachepetse pang’ono?”

Anaganiza kwa mphindi imodzi ndipo kenaka anatsitsapo. “Kodi mungasunge cheke mpaka Lachiwiri musadakatenge ndarama zake?” Ndidafunsa. Iye anati, “Palibe vuto,” ndipo ndinalimba chekecho. Munalibe ndarama mu *account* Lachisanu limenelo, ndipo sindimadziwa kuti zidzakhalako bwanji Lachiwiri lisanafike, koma magetsi adakhalabe mpaka kumapeto kwa sabata. Sindikukumbukira zomwe ndidachita Lachiwiri, koma mwina ndidapezapo chinthu choti ndigulitse.

Ili linali tsiku lina mmoyo wathu tikukhala mmavuto azachuma. Tsopano lingalirani kukhala motere kwa zaka zisanu ndi zinayi! Kukhala pansu pa zovuta zotere kumaimitsa masomphenya onse ndikuchotsa chisangalalo chilichonse chomwe chingabwere tsiku ndi tsiku. Lingaliro lililonse likuyang’ana pa kupulumuka, komwe mungapeze ndarama zolipira ngongole yotsatira. Kodi ndinawononga ndarama zambiri sabata yatha? Kodi nditenge chowerengera ndarama pokagula kuti ndisakapitirire pa zimene ndifuna kugula monga mwa ndarama zimene ndiri nazo? Nthawi zonse ndingoganizira momwe ndingachitire pogula zinthu mwa njira yotsika mtengo kwambiri. Mnzanga, mmenemo simomwe muyenera kukhalira! Onani zimene Mateyu 6:25 amanena.

Chifukwa chake ndinena kwa inu, Musadere nkhawa moyo wanu, chimene mudzadya ndi chimene mudzamwa; kapena thupi lanu, chimene mudzabvala. Kodi moyo suli woposa chakudya, ndi thupi loposa chovala?

— Mateyu 6:25

Yesu akunena kuti zinthu za moyo si moyo! Chilichonse pano cha mmoyo wathu chithandizira moyo, cholinga chathu. Koma popeza kuti Adamu anataya zofunikira za Ufumu, moyo unasinthidwa ndipo tsopano zonse zimene zimathandizira moyo nzofunika kwambiri kuposa moyo weniweniwo. Anthu sadziwa chimene moyo weniweniwo uliri ndipo sadziwa kuti iwo ndi ndani kwenikweni. Funsani aliyense kuti iwo ndi ndani ndipo adzakuzani zomwe akuchita. “Ine ndine dokotala, ndine *Realtor*,” ndi zina zotere. Ayi, sindicho chimene inu muli; ndi zomwe mumachita. Munthu wataya maloto ake. Zomwe ndikutanthauza ndikuti munthu tsopano akulota momwe angapangire ndarama zambiri koma wataya maloto a cholinga. Mwakunena kwina, chilichonse chomwe amalipira ndarama zambiri chimakhala maloto ake. Komabe, chifukwa munthu aliyense adalengedwa mwapadera ndi mphatso ndi luso losiyana, amadzipeza ali pazochitika kapena ntchito yomwe sichokhumba chawo. Moyu umakhala wautali, kudikirira ufulu wocheza kumapeto kwa sabata, kapena moyo wautali wodikirira kupuma pantchito.

Ndiye ndikufunsi funso. Ngati mudakakhala osafuna ndarama, ndikukhala ndi ndarama zambiri kuposa zomwe mukhoza kugwiritsa ntchito mmoyo wanu, mukanatani? Mwina mudakabweretsa china chosiyana ndi chomwe mukuchita pakali pano.

Monga ndanena kale, ndikudziwa kuchokera ku ziwerengero kuti osachepera 70% aku America, atafunsidwa ngati amakonda ntchito yawo, adanena kuti sakuchita zomwe amakonda. Ndikufuna kuti mumvetse kuti kuthamangira chuma, kukakamizidwa kuchita, kudera nkhwawa za mawa silinali dongosolo la Mulungu pachiyambi.

Chotero Mulungu adalenga munthu mchifanizo chake, mchifanizo cha Mulungu adalenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi. Mulungu anawadalitsa, nati kwa iwo, “Mubalane muchuluke; mudzaze dziko lapansi muligonjetse. Mulamulire pa nsomba za m’nyanja ndi pa mbalame za m’mlengalenga ndi pa zamoyo zonse zakukwawa padziko lapansi.”

Ndipo Mulungu anati, “Ndakupatsani zomera zonse zobala mbewu padziko lonse lapansi ndiponso mtengo uliwonse wa zipatso zobala mbewu mmenemo. Zidzakhala chakudya chanu. Ndipo ndapatsa zinyama zonse za dziko lapansi ndi mbalame zonse za m’mlengalenga ndi zonse zakukwawa padziko lapansi—mmene muli moyo—therere laliwisi lonse likhale chakudya.” Ndipo kunatero.

Ndipo anazona Mulungu zonse zimene anazipanga, ndipo taonani zinali zabwino ndithu. Ndipo panali madzulo, ndipo panali mmawa—tsiku lachisanu ndi chimodzi.

— Genesis 1:27-31

Munthu analengedwa pa tsiku lachisanu ndi chimodzi la kulenga—pa mapeto a tsiku lachisanu ndi chimodzi, kunenetsa. Analengedwa kumapeto kwa tsiku lachisanu ndi chimodzi chifukwa analengedwa kuti azikhala ndi Mulungu pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, tsiku limene timalidziwa kuti ndi tsiku la mpumulo.

*Ndipo zinatha kupangidwa zakumwamba ndi dziko lapansi ndi khamu lawo lonse. Tsiku lachisanu ndi chiwiri Mulungu anamaliza ntchito yonse anaipanga; ndipo anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri ku ntchito yake yonse. Mulungu ndipo anadalitsa tsiku lachisanu nid chiwiri, naliyeretsa lime-
nelo, chifukwa limenelo anapuma ku ntchito yake yonse imene Mulungu anailenga ndi kupanga.*

— Genesis 2:1-3

Baibulo limanena kuti Mulungu anapuma pa tsiku la chisanu ndi chiwiri. Sanali wotopa! Iye anali atamaliza. Zonse zinali zangwiro. Chilichonse chimene munthu akadafuna padziko lapansi chinali kale pa dziko lapansi pamene munthu anaonekera. Mtendere! Munthu anali ndi zofunikira zonse zimene akadafuna. Panalibe kuda nkhawa ndi kulipira ngongole, panalibe kuda nkhawa chifukwa chodwala. Anali ndi thupi langwiro ndi mkazi wangwiro. Chinthu chokha chimene angaike maganizo paicho ndi kungoyang'anirana wina ndi mnzake, Mulungu, ndi ntchito yawo, kapena cholinga chawo. Adamu anali wolamulira dziko lapansi; analilamulira kotheratu ndi ulamuliro ndi mphamvu ya Ufumu wa Mulungu. Koma tikudziwa kale mmene nkhaniyo inathera. Adamu ndi Hava anapandukira Ufumu wa Mulungu ndipo

**CHUMA CHIMATIKOPERA
KU NJIRA YOTHAWIRA KU
MALO A MPUMULO—
MALO AMENE TINGAIKE
MAGANIZO ATHU PA
ZIMENE TIKUFUNADI
KUCHITA, KUKHALA
NDI MOYO WODZAZA
NDI CHOLINGA
MMALO MOKOFUNA
KUPULUMUKA.**

anataya udindo wawo, anataya zofunikira zawo, ndipo anataya cholinga chawo. Cholinga chawo chinakhala chimodzi chongoti apulumuke. Nkhawa ndi mantha tsopano zidawononga malingaliro awo ndi kulimbana koti apulumuke. Monga momwe Genesis 3:17 amanenera, zinafunikira ntchito yowawa ndi kukhetsa thukuta.

Adamu anataya tsiku lachisanu ndi chiwiri!

Panalibe mpumulo tsopano, panalibe mtendere. Mdimba osakhutitsidwa unakuta moyo wake, ndipo Adamu anayenera kuthamangathamanga kuti akhale patsogolo pa cholepheretsa chilichonse. Kuyambira nthawi imeneyo, munthu wakhala wosakhutitsidwa. Koma panali chiyembekezo. Pamene munthu anachimwa, Mulungu anampatsa iye chikumbutso, chithunzi ngati angafune, cha chimene Iye tsiku lina adzabwezeretsedwa ku chilengedwe Chake. Linatchedwa Sabata. Mawu akuti *sabata* kwenikweni amatanthauza kupumula. Tsiku lachisanu ndi chiwiri la sabata linaperekedwa kwa munthu ngati tsiku la Sabata. Chofunikira pa Sabata, monga momwe mungaganizire, chinali kusagwira ntchito; panalibe kukhetsa thukuta ndi ntchito zowawa zomwe zinkaloledwa. Linali tsiku limene munthu anayenera kukhala, kusangalala ndi banja lake, ndi kulambira Mulungu. Zofunikira zonse za pa Sabata zinayenera kumalizidwa Sabata lisanayambe. Ngakhale chakudya cha Sabata chimayenera kukonzedweratu tsikuli lisanafike. Linali tsiku lopumula lomwe lili ndi zonse zofunikira zokonzedwa kale. Munthu akhoza kuima ndi kuganiza za chinthu china osati kugopulumuka.

Tsiku la Sabata linali limenelo. Koma kuyambira nthawi imeneyo anthu akhala akulota za moyo wa mpumulo. Kufunafuna chuma kwa munthu ndi chizindikiro cha chikhumbo chake chofuna

kumasuka ku zowawa ndi zokhetsa thukuta zomwe zamumanga mu ndende moyo wake wonse. Chuma chimatikopera ku njira yothawira ku malo a mpumulo—malo amene tingaike maganizo athu pa zimene tikufunadi kuchita, kukhala ndi moyo wodzaza ndi cholinga mmalo mokofuna kupulumuka.

Lero, Sabata, tsiku lachisanu ndi chiwiri, kaya mumalikondw-erera pa Loweruka kapena Lamlungu, silimachitidwa ulemu waukulu mu chikhalidwe chathu. Inde, anthu ambiri amapita kutchalitchi Lamlungu mmawa. Komabe kuyang’ana chikhalidwe chonsecho, simungathe kuchisiyanitsa ndi zovuta zina pa tsiku logwira ntchito. Ndili mwana, zonse zimatsekedwa pa tsiku Lamlungu. Simukadatha kupita kukagula Lamlungu; kugula gasi Lamlungu. Bambo anga amaonetsetsa kuti agule gasi Loweruka madzulo kuti atsimikize kuti ali ndi zimene amafunikira Lamlungu. Ngati mumadziwa zambiri za ine, mukudziwa kuti ndimakonda kusaka, koma monga wosaka, sindikanatha kusaka Lamlungu. Kusaka Lamlungu kunali koletsedwa. Anthu anali kukonda kuvala zovala zawo zabwino kwambiri komanso kudyia chakudya pamodzi Lamlungu. Koma ndithudi izo zonse zasintha lero. Koma chithunzi chenicheni cha Sabata sichinatero.

Ngakhale kuti Sabata linali lokonzedwa bwino chotani, ngakhale kuti chakudya cha banja chinali chachikulu motani, Lolemba linali kubwera. Mawu akuti “mavuto a pa Lolemba mmawa” akhala akufanana ndi liwu lakuti *choopsa* kwa nthawi yonse yomwe ndikukumbukira. “Ndiyenera kupita kuntchito” ndi “kubwerera ku ntchito pakutha tchuthi” anali mawu amene anali kugwiritsidwa ntchito kufotokoza Lolemba mmawa. Ndipo ngati mukaganizira, zinali kungomveka ngati ukapolo. Koma zikomo Mulungu ndi Lachisanu! Ngakhale lerolino, Loweruka ndi Lamlungu limapereka

malo opumula kwa kanthawi kochepa kwa anthu ambiri. Koma kuchuluka kwa magalimoto pa Lolemba mmawa kumakhala kuli kuyembekezera.

Koma bwanji padakakhala njira yeniyeni yokhala umoyo monga mu Sabata kwa nthawi zonse. Kukanakhala kodabwitsa chotani ngati pakanakhiladi njira yokhalira moyo wopanda mantha, wodzala ndi zofunikira, wodzaza ndi cholinga, ndi kukhala mmalo a mpumulo! Drenda ndi ine tinakhala moyo wa chizunzo, mantha, matenda, ndi kusatetezeka kwa zaka zisanu ndi zinayi mpaka pamene tinapeza kuti mpumulo wa Sabata unali mwayi kwa miyoyo yathu. Ndikunenetsa!

Momwemo, utatsalira, mpumulo wa Sabata kwa anthu a Mulungu; pakuti iye amene adalowa mpumulo wake adapumulanso mwiniwake ku ntchito zake, monganso Mulungu ku zake za Iye. Chifukwa chake, tichite changu chakulowa mpumulowo, kuti wina angagwe m'chitsanzo chomwe cha kusamvera.

— Aheberi 4:9-11

Mzanga, ichi ndi Chipangano Chatsopano. Pali mpumulo wa Sabata womwe ulipo kwa anthu a Mulungu lero. Lembo limeneli likusonyeza kuti tingalowe mu mpumulo wa Mulungu mwakupumula ku ntchito yathu. Kumbukirani zomwe tangophunzira kumene: Mpumulo wa Mulungu umati zonse ndi zathunthu, zokwanira, ndi zofunukira zilipo. Pali ufulu kuchoka ku maganizo ongopulumuka, ukapolo wanjala, matenda ndi nthenda. Pali mwayi watsopano! Sabata sichinali chidziwitso cha Chipangano Chakale, ndi cha ifenso lero.

Koma musanaganize kuti ndikukamba za kukhala pansu pa

malamulo ndi miyambo ya Chipangano Chakale, sindikutero. Mmalo mwake, ndikufuna ndione mpumulo wa Sabata uwu umene Aheberi amakamba. Chifukwa chakuti monga momwe ine ndi Drenda taonera, mmenemo muli fungulo yofunika kwambiri ya Ufumu wa Mulungu kugwira ntchito ndi kupereka mmiyoyo yathu monga momwe Mulungu anafunira.

**KUKANAKHALA
KODABWITSA CHOTANI NGATI
PAKANAKHALADI NJIRA
YOKHALIRA MOYO WOPANDA
MANTHA, WODZALA NDI
ZOFUNIKIRA, WODZAZA NDI
CHOLINGA, NDI KUKHALA
MMALO A MPUMULO!**

CHODABWITSA: SABATA SITSIKU LIMENELONSO!

Ndiganiza kuti fundo iyo yakukopani. Pakhala kukambirana mu mpingo wa Yesu kuti Sabata lisungidwe bwanji: Loweruka, Sabata, kapena kuyamba pakulowa dzuwa pa Chisanu usiku mpaka kulowa dzuwa kwa Loweruka madzulo. Mipingo yonse inamangika pakutanthauza kwa pa Sabata. Musanataye buku ili ndi kuganiza kuti ndine wachiphunzitso chonyenga, pirirani nane pang'ono, tiyeni tione pa Akolose 2:16-17.

Chifukwa chake munthu aliyense asakuweruzeni inu m'chakudya kapena chakumwa, kapena m'kunena tsiku la phwando, kapena tsiku lokhala mwezi kapena la Sabata. Ndizo mthunzi wa zili nkudzazo; koma thupi ndi la Kristu.

— Akolose 2:16-17

Samalirani kwambiri zimene Paulo akunena. Tsiku la Sabata ndilo mthunzi wa zili nkudzazo; koma thupi ndi la Kristu. Tsiku la Sabata linali mthunzi, sichinali chenicheni. Ngati Kristu ali chinthu chenicheni, ndiye kuti tsiku la Sabata linali mthunzi wa yemwe Iye ali ndi zomwe Iye anachita. Ndiloreni ndinene motere: Palibe mphamvu mu tsiku la Sabata yochotsa kapena kusintha dongosolo la temberero la dziko lapansi la ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta limene Adamu anabweretsa padziko lapansi. Ngati mulilemekeza mwachipembedzo, mwa ilo lokha komanso mwalokha, mulibe mphamvu yokumasulani. Koma ndi mthunzi, chithunzi, cha zomwe mudzapeza mwa Kristu.

Pamene ndinali mu *grade* yoyamba, mphunzitsi wanga anatiuza kuti tonse tijambule mitu yathu chammali. Anatenga *projector* nkutikhazika kutsogolo kwake, ndipo inali kuika mthunzi wa mitu yathu papepala loyera. Kenako adajambula cholozera chamithunzi yathu ndikupanga mitu yathu, yomwe tidadula ndikupita nayo kunyumba kwa amayi athu kukawapatsa pa Tsiku la Amayi. Mthunziwo unaonetsa zina za ine, koma sunagwire zenizeni momwe ndiliri, khalidwe langa, kapena umunthu wanga. Koma udapereka chidziwitso china za ine.

Tsiku la Sabata lionetsa chimodzimodzi. Mthunzi wake unenedwa kuti sugwira ntchito, palibe zowawa komanso kukhetsa thukuta. Unali mthunzi chabe, komabe, osati weniweni. Koma unali kuloza kwa Yesu Kristu, amene, kwenikweni, watimasula ku temberero la chilamulo ndi dongosolo la temberero la dziko lapansi ndikutikhazikitsanso monga ana aamuna ndi aakazi a Mulungu ndi nzika za Ufumu waukulu wa Mulungu! Apanso, chinali chithunzi cha zomwe Yesu adzatibweretsera tsiku lina. Ndi ntchito yomalizidwa kumene zonse zomwe zimafunikira pamoyo zabwezeretsedwa

kwa ife. Komabe, monga momwe Aheberi amanenera, timalowa mu mpumulo umenewu mwa chikhulupiriro. Kumbukirani, chikhulupiriro chimafunikira kuti kumwamba kukhale ndi ulamuliro pano padziko lapansi. Pa mtanda Yesu anafuula kuti: “Kwatha! monga Mulungu ananenera kuti kunatha kumapeto kwa tsiku lachisanu ndi chimodzi.

Sabata kwa anthu ambiri lero ndi tsiku lachipembedzo. Anthu amaona Sabata ngati tsiku la Mulungu, tsiku limene tiyenera kupita kutchalitchi, kuchitira Mulungu zinthu, ndi kuchita zinthu zina zachipembedzo. Yesu anayenera kukonza ophunzira Ake, omwe anali ndi maganizo ofanana.

Sabata linaikidwa chifukwa cha munthu, si munthu chifukwa cha Sabata.

— Maliko 2:27

Sabata linaikidwa chifukwa cha munthu, si munthu chifukwa cha Sabata. Kodi mukudziwa kuti anthu ambiri amadziimba mlandu ngati sanapite kutchalitchi? Kodi ndi chifukwa chiani amadziimba mlandu posapita ku tchalitchi pamene iwo ali ndi tchalitchi? Sindi-kunena kuti tisamasonkhane pamodzi mkupembedza konse, koma maganizo amaonetsa kuti ali ndi kuona kolakwika paza Sabata.

Ndikudziwa kuti mungakhalebe osokonezeka, ndiye ndiloreni ndizame poyang’ana ndemanga yomwe Yesu ananena mu Yohane 11.

Ndipo pamene Yesu anadza, anapeza kuti pamenepo atakhala kale m’manda masiku anayi. Koma Betaniya anali pafupi pa Yerusalemu, nthawi yake yonga mastadiya khumi

ndi asanu, koma ambiri a mwa Ayuda anadza kwa Marita ndi Mariya kudzawatonthoza mtima pa mlongo wawo. Pamenepo Marita pakumva kuti Yesu ali nkudza, anamuka kukakumana ndi Iye, koma Mariya anakhalabe m'nyumba.

Ndipo Marita anati kwa Yesu, “Ambuye, mukadakhala kuno, mlongo wanga sadakafa.

Koma ngakhale tsopano ndidziwa kuti zinthu zili zonse mukapempha Mulungu, adzakupatsani Mulungu” Yesu ananena naye, “mlongo wako adzauka.” Malita ananena ndi Iye, “ndidziwa kuti adzauka mkuuka tsiku lomaliza.”

Yesu anati kwa iye, “Ine ndine kuuka ndi moyo. Wokhulupirira Ine ngakhale amwalira adzakhala ndi moyo; ndipo yense wakukhala ndi moyo, nakhulupirira Ine, sadzamwalira nthawi yonse. Kodi ukukhulupirira ichi?”

Ananena ndi Iye, “Inde, Ambuye, ndakhulupirira kuti Inu ndinu Kristu, Mwana wa Mulungu, wakudza m'dziko lapansi.”

— Yohane 11:17-27

Yesu anati Iye anali chiukitso; sichinali cha tsiku lokhalo. Tsiku la Sabata linali mthunzi wa zimene Yesu anachita pa mtanda chifukwa cha ife. Yesu ndiye Sabata yeniyeni ndipo mwa Iye timapeza mwayi wolowa mu Ufumu wa Mulungu ndi zonse zomwe uli nazo. Motero, tikhoza kupumula!

Choncho tiyeni tibwererenso ku Lembo la Chipangano Chatsopano mu Aheberi.

Momwemo, utatsalira, mpumulo wa Sabata kwa anthu a Mulungu; pakuti iye amene adalowa mpumulo wake

adapumulanso mwiniwake ku ntchito zake, monganso Mulungu ku zake za Iye. Chifukwa chake, tichite changu chakulowa mpumulowo, kuti wina angagwe m'chitsanzo chomwe cha kusamvera.

— Aheberi 4:9-11

Mthunzi wa tsiku la Sabata ukunenedwa kuti ndikoletsedwa kwa inu kugwira ntchito ndi kuthetsa thukuta pa zomwe mukufuna pa tsiku la Sabata, koma kunali kungotipatsa chithunzithunzi cha zomwe Yesu adachita, zomwe zinali kutimasula ku dongosolo la temberero la padziko lapansi loti tiyenera kuvutika ndikukhetsa thukuta kuti tipulumuke. Mwa kuyankhula kwina, zomwe zinaonetsedwa zidakhala zenizeni mwa Kristu. Ndipotu uthenga woyamba umene Yesu analalikira unali onena za tsiku la Sabata. Mu Yesaya 61, timapeza mawu a ulaliki Wake woyamba, umene Iye analalikira mu Luka 4.

Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine, chifukwa Yehova wandidzoza kuti ndilalikire uthenga wabwino kwa osauka.

— Yesaya 61:1

Mwa kunena kuti pali njira yochotsera umphawi, iye anali kunena kuti pali njira yotulukira mu dongosolo la temberero la dziko lapansi padziko la ntchito zowawa ndikukhetsa thukuta. Unali ukapolo wopezera zinthu zofunikira umene unachititsa anthu ukapolo wopezera mpumulo. Koma tsiku la Sabata silinali chithunzi chokhacho chimene Mulungu anapereka kwa anthu Ake cha zimene zidzabwezeretsedwe tsiku lina. Panalinso chaka cha Sabata!

Pakutha pake pa zaka zisanu ndi ziwiri pakhale chilekerero. Chilekererocho ndi ichi: Okongoletsa onse alekerere chokongoletsa mnasi wake asachifunse kwa mnasi wake kapena m'bale wake, popeza analalikira chilekerero cha Yehova. Muyenera kuchifunsa kwa mlendo, koma chanu chilichonse chili ndi m'bale wanu dzanja lanu lichilekerere.

Ndiko kuti pasakhale waumphawi mwa inu, pakuti Yehova adzakudalitsani kwambiri m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale cholowa chanu chanu, chokhachi mumvere chimverere mawu a Yehova Mulungu wanu kuti musamalire kuchita malamulo awa onse amene ndikuuzani lero lino. Popeza Yehova Mulungu wanu adzakudalitsani monga ananena nanu, ndipo mudzakongoletsa amitundu ambiri osakongola nokha. Nimudzachita ufumu pa amitundu ambiri koma iwo sadzachita ufumu pa inu.

— Deuteronomo 15:1-6

Onani kuti anafunika kuchotsa ngongole pa zaka zisanu ndi ziwiri zilizonse. Apanso tikuona Mulungu akugwiritsa ntchito nambala ya zisanu ndi ziwiri kusonyeza kuti zonse zatha. Palibe chosowa; Iye wapereka zonse zofunika kwa munthu. Koma ngati anafunsa nzeru Zake pakuwauza zakukhululukira ngongole, Iye anawonjezera kuti: **“Ndiko kuti pasakhale waumphawi mwa inu, pakuti Yehova adzakudalitsani kwambiri m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale cholowa chanu chanu.”** Anapitiriza kunena kuti iwo anayenera kudalitsidwa kwambiri moti adzakhala okongoletsa osakongola okha. Apanso tikuona kuti dongosolo la temberero a dziko lapansi la ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta linathetsedwa ndi lamulo latsopano la moyo limene linatichotsa ku temberero la lamulo cha uchimo ndi imfa.

Monga pa tsiku la Sabata, sanafunikire kugwira ntchito yowawa ndi yokhetsa thukuta kwa chaka chonse; motero, sanaloledwa kufesa mbewu zawo. Koma kenako zinthu zinafika potopetsa. Osati kokha kuti akhululukire ngongole iliyonse imene wina anali nayo kwa iwo, komanso sanali kuloledwa kufesa mbewu zawo. Panthawiyi, wina anganene kuti, “Ayi, ndikhoza kukhala ndi moyo tsiku limodzi ndi zomwe zili mu firiji, koma kupulumuka chaka chonse osagwira ntchito kumakhala kovuta kwambiri.”

Ndiye apanso, mthunzi ukutiuzza kuti tikhulukire angongole athu. Iye anawauza kuti sayenera kugwiritsa ntchito ngongole chifukwa adzakhala ndi zambiri moti adzakhala okongoletsa osakongola okha. Ngongole ndi dongosolo lobwera chifukwa cha kusakwanira kwa zofunikira, koma Mulungu adzapereka zonse kwa iwo kotero kuti ngongole sidzafunikanso. Mthunzi umati, “Usabzale mbewu zako,” kutanthauza njira yatsopano yakukhala kunja kwa dongosolo la temberero la dziko lapansi. Tsopano, zonsezi zimapezeka mwa Yesu Kristu.

Koma dikirani, chilipo chinanso—chithunzi chachikulu kwambiri chosonyeza anthu a Mulungu chimene chinali nkudza. Chinali kutchidwa Chaka Choliza Lipenga.

MUTU 7

IZI NDI ZOSATHEKA!

Zomwe mukufuna kuwerenga ndizodabwitsa. Ayi, ndiloreni ndifotokozenso izi. Mudzaganiza kuti ndi zosatheka konse. Ndikunena za Chaka Choliza Lipenga (cha makumi asanu), chithunzi chachikulu cha zomwe Yesu akufuna kuchita mu chuma chanu cholembedwa mu Chipangano Chakale, komabe ndi anthu ochepa amene amadziwa kapena kumvetsa zomwe akunena. Talankhula kale za tsiku la Sabata ndi chaka cha Sabata, zonse zomwe zili mithunzi ya zomwe tili nazo mwa Kristu, koma tsopano tabwera ku chochitika chachikulu, Chaka Choliza Lipenga.

Dzinali likumveka ngati chikondwerero, sichoncho? Komabe, pankhani ya zachuma, anthu ambiri—ndipo ndimati anthu ambiri, ndi zomvetsa chisoni, izi zikutanthauza kuti Akristu ambiri, nawonso—alibe zambiri zoti azikondwerera. Monga ndidanena, ndakhala wochitachita pantchito ya zachuma kwa zaka makumi atatu mphambu zisanu ndi chimodzi tsopano. Ndili ndi ma *company* angapo tsopano ndipo ndimagwira ntchito ndi anthu ambirimbiri pa zachuma zawo panthawi yomweyo. Kotero ine ndikudziwa zomwe zili kunja uko. Nthawi zambiri ndimadziwa zomwe zimachitika kuseri kwa galimoto yatsopano yonyezimira

kapena nyumba yabwino kwambiri. Nthawi zambiri zimakhala ndi ngongole zambiri komanso nkhawa. Eya, sindikuti kukhala ndi galimoto yabwino kapena nyumba yaikulu ndikoipa. Zimafuna ndarama zambiri lero kuti mukhale ndi moyo.

Ndipo dongosolo la temberero la dziko lapansi ndi njira yopulumukira yomwe nthawi zambiri imalephera kumasula anthu. Ndikhulupirireni, mwa zikwi ndi zikwi za anthu omwe ndakumana nawo, ambiri sanali anthu oipa. Iwo anali kuchita zonse zimene akanatha paokha, ndipo sanali kudziwa za Ufumu wa Mulungu kapena zimene ndikugawira mbukuli. Zoonadi, mukudziwa kuti ine ndi Drenda tinali kukhala moyo wopanikizika pa ndarama kwa zaka zisanu ndi zinayi mpaka titaphunzira za mpumulo wa Sabata. Titakhala ndi moyo wotero kwa nthawi yaitali, simuzindikira kuchuluka kwa zovuta zomwe mumakumana nazo ndikuganiza kuti ndizabwinobwino.

Zaka zingapo zapitazo, Mulungu anachita nane za kaganizidwe kanga kakang'ono ndipo anandiuza kuti ndiyenera kusangalala ndi kuliza Lipenga, phwando, koma sindinatero. Inde, ndinalibe ngongole; inde, ndinaona zinthu zodabwitsa zikuchitika; ndipo inde, ndinali wokondwa komanso wokhutira. Koma ndinasiya kulota ndipo Mulungu anachidziwa, ndipo anali kufuna kuti ndipitirizenso, mwakuchita zina ndi kulota. Ndinali nditakalamba pang'ono, komabe ngakhale ndinali wokalamba ndinali wokondwa.

Monga ndidanenera, ndili ndi *company* ya zachuma, ndipo ndimaitanidwa chaka chilichonse, ndi mmodzi wa amalonda wanga, ku chikondwerero cha kuchita bwino pa malonda a chaka chopita. Ofika nthawi zambiri amakhala pafupi 250 apamwamba komanso akuluakulu. Unali ulendo wolipiriratu ndarama zonse kupita kumalo ena abwino kwambiri, koma kwa ochepa kwambiri, panali

kulemekeza kwapadera ndi macheke a bonasi. Chifukwa chakuti ndinali wotanganika ndi ubusa wa tchalitchi chachikulu, kuchita TV, ndi kuyendetsa *company* yanga, nthawi zonse ndimadziwa kuti ndinalibe nthawi yochita ntchito yofunikira kuti ndifike pamlingo wapamwamba wachilemekezo chotero.

Koma chaka china, nditakhala mumsonkhano ndikuona anzanga khumi apamwamba akulemekezedwa ndikulandira macheke awo a bonasi ya \$100,000, ndinatsutsika. Ndinaganiza, “Dikirani pang’ono! Ndiyenera kukhala pamwamba pa nsanja imeneyo ndikulemekezedwanso. Ndine mwana wa Mulungu ndipo Mzimu Woyera ndi Mlangizi wanga. ’Ndiyenera kukhala kumeneko ndikugawana ndi kusonyeza ubwino wa Mulungu!’” Chifukwa chake ine ndi Drenda tinatsimikiza nthawi yomweyo kuti tidzakhala pa nsanja imeneyo chaka chamawa. Bwanji? Sitinadziwe njira yake.

Kwa zaka khumi zapitazi, ndakhala ndikuchita pafupifupi \$3 mpaka \$4 *million* pachaka ndi *company* imodziyi, koma zotsatira zake kuti ndikhale mmodzi wa khumi oyambirira pamanikira \$11 *million*. Sindinadziwe kuti ndidzafika bwanji pamlingo umenewo ndipo sindinali otsimikiza kuti zikadatheka ndi dongosolo langa. Chinthu chimodzi chimene ndinaphunzira chinali chakuti sindinathe kuchichita mwa mphamvu zanga. Motero ine ndi Drenda tinapemphera ndi kukhazikitsa cholinga chathu, kufesa mbewu yandarama, kumasula chikhulupiriro chathu, ndi kuchitcha kuti chachitika.

Kuti tifotokoze mwachidule, mu January wa chaka chime-necho, pamene chaka chatsopano chinali chitangoyamba kumene, Mulungu anandionetsa mmene ndingakwaniritsire cholinga changa mmaloto. Anandisonyeza zenizeni zomwe ndimayenera kuchita; ndipo ndidakachita zenizeni zomwe adandionetsa, zonse

zinali zotheke. Kodi mukudziwa kuti tidapanga \$11 *million* chaka chimenecho ndikugulitsa kamodzi! Zinali zosangalatsa kukhala

**SIMUZINDIKIRA
KUCHULUKA KWA
ZOVUTA ZOMWE
MUMAKUMANA NAZO
NDIKUGANIZA KUTI
NDIZABWINOBWINO.**

pa nsanja imeneyo pamsonkhano wotsatira monga mmodzi wa anthu khumi a mu *company* ndikulandira chilemekezo cha \$100,000. Kodi mukufuna kudziwa kuti zinamveka bwanji? Chikondwerero chachikulu. Osati kongofikitsa ku cholinga chathu cha chilemekezo chokha, koma ndarama zathu zolowa zinakwera kwambiri chaka chime-

necho. Zikumveka monga chikondwerero kwa ine!

Chifukwa chake ndikayamba kunena za chochitika china cha Chipangano Chakale ngati Chaka Choliza Lipenga, osawodzera ndikuganiza kuti izi ndi zinthu zotopetsa popeza sichoncho. Kumbukirani, moyo umayenda bwino ndi chikondwerero, kotero tiyeni tione chochitika pa chikondwerero chomwe Israyeli adasangalala ndikuphunzira momwe mungachitire chanu.

Chaka Choliza Lipenga

Ndipo uziwerengera masabata a zaka asanu ndi awiri— zaka zisanu ndi ziwiri kasanu ndi kawiri—kotero kuti zaka zamasabata asanu ndi awiri zifikire zaka makumi anayi kudza zisanu ndi zinayi. Pamenepo uzitumizira lipenga lomveka mwezi wachisanu ndi chiwiri tsiku la khumi la mweziwo; Tsiku la chitetezero mutumizire lipenga lifikire

m'dziko lanu lonse. Ndipo muchipatule chaka cha makumi asanu ndi kulalikirira kwa onse okhala m'dziko kuti akhale afulu. Muchiyese chaka choliza lipenga; ndipo mubwerere munthu aliyense ku zakezake ndipo mubwerere yense ku banja lake. Muchiyese chaka chamakumi asanucho choliza lipenga, musamabzala, kapena kucheka zophuka zokhala mmenemo; kapena kucheka mpesa zake zamipesa yosadzombola. Popeza ndicho chaka choliza lipenga muchiyese chopatulika; mudye zipatso zake kunja kwa munda. Chaka Choliza Lipenga ichi mubwerere nonse ku zakezake.

— Levitiko 25:8-13

Pamene ndiyamba kukamba za Chaka Choliza Lipenga, ndiloreni ndikhasikitse fundo zimene mwazizindikira kale. Chaka Choliza Lipenga chinali kuchitika pa zaka zilizonse za makumi asanu, ndipo chinali kuchitika chitangotha chaka cha sabata, chaka cha makumi anayi kudza zisanu ndi zinayi. Ndikuganiza kuti mutha kuona kale vuto lalikulu likubwera, sichoncho? Mu chaka cha Sabata, Israyeli sanali kuloledwa kubzala mbewu zawo. Chaka Choliza Lipenga kutsatira chaka chimenecho panali ndi lamulo lomweli la kusabzala mbewu. Chotero, Israyeli sanakolole kwa zaka ziwiri zotsatizana ndipo anayembekezera m'chaka chachitatu kuti mbewuzo zikhwime ndi kukololedwa kuti zikhalenso chakudya chawo. Limeneli likhoza kukhala vuto lalikulu kwa aliyense amene anali kukonda kudya chakudya chabwino kapena amene anali kupeza ndarama pogulitsa tirigu. Pamene Mose anapereka malangizo okhudza Chaka Choliza Lipenga, mungaganizire chisokonezo chimene chinayambika. Zoonadi, ganizo lokhala

zaka zitatu zopuma linali lingaliro labwino, koma wina amayenera kulipira. Chinthu choyamba chimene anafunsa Mose atamva zimenezi chinali chakuti, “Zingatheke bwanji?”

Ndipo mukadzati, “Tidzadyanji mu chaka cha chisanu ndi chiwiri taonani sitidzabzala sitidzakolola zinthu?” pamenepo ndidzauza dalitso langa litsika pa inu chaka chachisanu ndi chimodzi, ndipo chidzapatsa zipatso zofikira zaka zitatu. Ndipo mubzale chaka chachisanu ndi chitatu, ndikudya zipatso zasundwe kufikira chaka cha chisanu ndi chinayi mpaka zitacha zipatso zake mudzadya zasundwe.

— Levitiko 25:20-22

Mulungu adawayankha yankho lodabwitsa lomwe tikhala nthawi yaitali tikulisanthula gawo lomaliza la bukuli. Iye ananena kuti adzatumiza madalitso oterowo m’chaka chachisanu ndi chimodzi mwakuti adzapereka zokolola zokwanira zaka zitatu kufikira kukolola kwatsopano kudzafika pambuyo pa Chaka Choliza Lipenga. Pali kusiyana pamenepa ponena za masiku a chilengedwe. Baibulo limanena kuti Mulungu anatha pa tsiku lachisanu ndi chimodzi la kulenga ndipo anapumula. Ngakhale anapumula, sanatope. Mmalo mwake, Iye anatsiriza. Chilichonse chimene munthu amafuna chinalengedwa ndipo chinalipo kwa iye.

Tsopano Mulungu anali kusonyeza Israyeli chithunzithunzi cha kukhala ndi zokwanira koposa, zomwe zikusiyana kwambiri ndi dongosolo la temberero la dziko lapansi la ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta. Iye anali kufuna kuti iwo amuone Iye monga wowapatsa ndi kuzindikira kuti Iye amapereka zofunikira zamphamvu. Ndiponso, ngakhale kuti ichi chinali chithunzi kwa

iwo ku zofunikira za Mulungu mu tsiku lawo, sizinali kufikira mpaka pomwe Yesu anadza pamene ife tiona zomwe mthunzi unali kutisonyeza. Mwachilengedwe, panalibe njira yopulumukira zaka zituzo popanda kufesa mbewu. Momwemonso, mwachilengedwe, kukhala pansi pa dongosolo la temberero la dziko lapansi sipakana-khala njira yopezera ndarama popanda kuiwononga usana ndi usiku. Simungathe kuthamangathamanga mokwanira kuti zichitike. Yesani kutenga zaka zitatu pa tchuthi pa ntchito yanu yomwe muli nayo panopa ndi zanu zoyenera kuchita, mudzalawa umphawi. Koma Mulungu akuyesetsa kuwasonyeza chithunzi cha njira yatsopano, imene amapezera anthu ake zinthu zofunika pamoyo, monga mmene Adamu anapatsidwira zinthu zonse zimene Mulungu anamukonzera mnthawi yolenga zinthu.

Palinso zinthu zina ziwiri zimene Chaka Choliza Lipenga chimatisonyeza zimene tiyenera kuziona. Apanso tikuona nthaka ikupuma, osatopa ndi kukhetsa thukuta mu chaka chamakumi asanu ichi. Mudzaonanso kuti nthaka yonse inayenera kubwezedwa kwa mwini wake woyamba. Pamene Aisrayeli anawoloka Mtsinje wa Yordano, fuko lililonse ndi banja lililonse linapatsidwa nthaka imene inakhala yawo kuti alime ndi kupanga chakudya ndi kupeza ndarama zimene anafunikira kuti apulumuke nazo. Kunena zoono, nthaka inali chuma chawo. Mmenemo anali kulima mbewu ndi kuweta ziweto zawo. Chotero kuti nthaka yonse ibwezedwe kwa mwini wake woyamba kunali kubwezera mphamvu yolemerera.

Apanso, ndi mthunzi wachimene Yesu anatichitira. Mthunzi ukuti kulemera kunabwezedwa ku nzika za dziko la Aisrayeli. Choonadi chiteronso kwa ife, kuti kulemera kwathu kwabwezedwa kwa ifenso kuti umwini wa Ufumu wa Mulungu ndi wathunso.

Pali chinthu chachitatu chomwe Chaka Choliza Lipenga

chimationetsa, ndicho kuti akapolo onse anamasulidwa ndikubw-
erera ku mabanja awo. Ichi ndi chachikulu. Apanso, mthunzi ukunena
kuti sulinso kapolo koma mwana wamwamuna kapena wamkazi

**MUTAPHUNZIRA
ZOMWE SABATA
LIKUTIONETSA,
KUSINTHA
KWAKUKULU
KUNGACHITIKE
MMOYO WANU WA
ZACHUMA.**

mnyumba ya Mulungu. Choonadi mwa
Kristu chimanena kuti sulinso kapolo
koma mwana wamwamuna kapena
wamkazi mnyumba ya Mulungu koma
wokhala ndi ufulu wonse ku umwini
ndi kukulemera kwa nyumbayo.

Choncho ganizirani zimene
mwaphunzira kumene. Yesu anatib-
wezera zimene Adamu anataya. Yesu
anatomasula ku ukapolo, kutipanga
kukhala ana aamuna ndi aakazi a
Mulungu. Anatomasula ku dongosolo la

temberero la dziko lapansi la ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta,
kulola kuti Mulungu adalitse ntchito ya manja athu mwa njira ya
mphamvu. Ngakhale kuti Yesu analipira zinthu zonsezi, tiyenerabe
kudziwa mmene tingawiritsire ntchito zinthu zimenezi mmiyoyo
yathu yeniyeni ya dziko lapansi. Apatu ndi pamene Akristu ambiri
amaphonya. Posadziwa kuti Ufumu umagwira ntchito motsatira
malamulo, osadziwa ufulu wawo walamulo monga ana aamuna ndi
aakazi ndiponso nzika, amakhulupirira kuti Mulungu amasankha
yekha amene akufuna kudalitsa. Chotero, iwo samaphunzira
malamulo a Ufumu, amene ali ndi mafungulo a kusangalala ndi
akugwiritsira ntchito zimene Baibulo limanena kuti ndi zawo.
Ndikukuuzani, mutaphunzira zomwe Sabata likutionetsa, kusintha
kwakukulu kungachitike mmoyo wanu wa zachuma.

Mwamuna wina wa mumpingo wanga anayamba kundimva

ndikuphunzitsa za chikhulupiriro ndi mmene Ufumu wa Mulungu ukugwirira ntchito. Banja lake ndi ana ake anaphunzira malamulo amenewa pamodzi monga banja. Pamene chaka chatsopano chinali kuyandikira, anaganiza zoti agwiritse ntchito ufulu wawo wa ulamulo ndipo akukhulupirira kuti adzalipira malo awiri a *rent* omwe anangopeza kumene chaka chimenecho. Ngati ndikukumbukira bwino, ndikuganiza kuti ndarama zonse zomwe zimayenera kulipira nyumba zonse zinali pafupifupi \$400,000. Chifukwa chake adapemphera ndikufesa mbewu yaikulu yandarama ku cholinga cholipira nyumba zonse ziwiri mchaka chimenecho. Izi zinali zowawa kwambiri, koma mwamuna ameneyu anagwira ntchito m'munda momwe munali motheka kupeza amalonda okwanira komanso mapangano akuluakulu amalonda omwe atha kulipira mwayi wotero. Banja lonse lidapemphera pamodzi ndikuvomereza kuti izi zichitika. Mlungu uliwonse, banjalo linali kubwerazanso cholinga chawocho ndi kukambirananso Malembo amene anawapatsa ufulu wakuyembekezera zokololazo. Inde, mwamunayu anadziwa kuti ayenera kuchita mbali yake.

Chabwino popitirira chaka, ndithudi, mapangano akuluakulu ochepa adakhala otheka, ndi ma *company* akuluakulu koma okhudzana ndi ndarama za madola ma *million* ambiri sanakwaniritsidwa mwamsanga. Pafupifupi theka la chaka, mwamuna uyu adapeza ndikugulitsa malonda ambiri ku *company* yake, yaikulu kwambiri kotero kuti idatenga pafupifupi 40% yazinthu zonse zomwe *company*yake idapanga mchakachi. Ndi cheke cha *commission* imeneyo, anatha kulipira amodzi mwa malo a *rent*. Chakumapeto kwa chaka, *company* ina inanena kuti iwo adzasainadi mapangano a madola ama *million* ambiri omwe mnzanga amawapatsanso. Koma tsiku loti mgwirizanowo uchitike limasunthidwa. Zolembazo

zikakonzedwa, kenako tsiku limasunthidwa ndipo zolembazo zikukonzedwanso, tsiku limasunthidwanso. Tsopano inali nthawi yophukira mitengo pomwe mnzangayo adauzidwa kuti oyang'anira gulu lomwe amagwira nawo ntchito lasinthidwa ndipo gulu latsopano liyenera kulowa mmalo.

Mnzanga anatha mphamvu; anadziwa chimene ichi chimatanthauza. Gulu loyang'anira lomwe likubwera silinadziwe za pangano lomwe likuyembekezeka, lomwe tsopano linakhala ngati lopanda ntchito. Ayenera kuyambitsanso ntchitoyi ndi gulu latsopano. Pamene adakumana ndi gulu latsopano loyang'anira, adaoneka kuti adakonda malingaliro a *company* yake. Ataunikanso kumapeto kwa November, adati akufuna kupita patsogolo. Komanso, zolembalemba zinachedwa mpaka patakhala masiku awiri kuti chaka chatsopano chifike. Mnzangayo analandira foni kuti akufuna kukumana kuti asaine zolembedwazo, ndipo adzakhala akulipira ndarama ngati angakumane nawo ndikusaina tsikulo. Bwenzi langa linapanga ntchito yokwanira pa mgwirizanowo kuti akwaniritse cholinga chake cholipira nyumba zonse ziwiri mchaka chomwe iye ndi banja lake adaika chikhulupiriro chawo.

Kunali mwa kuphunzira fundo za Ufumu kumene kunamulola kapena kumsonkhezera ku cholinga chapamwamba choterocho, popeza asanakhalepo ndi *account* yaikulu chotero kapena kupanga ndarama zochuluka chotero mchaka chilichonse chakumbuyo zimene zikanasonyeza kuti cholinga chake chinali chotheka. Anandiuzadi kuti anali ndi phwando lalikulu lokondwerera kupambana kumeneko!

Nkhani ina, “zinachitikadi” zinachitika ndi mmodzi wa ana anga. Inde, ana anga onse aona Ufumu ukugwira ntchito mmoyo wawo wonse. Onse akugwiritsa ntchito fundo zimene ndikunenazi

ndipo aona Mulungu akuchita zinthu zodabwitsa. Ngakhale ali mzaka za makumi awiri, onse ali ndi magalimoto ndi nyumba zogulidwiratu mopanda ngongole ngati zilipo koma ndi zochepa. Mwana wanga wamwamuna wamkulu, Tim, anali kufuna kugula nyumba. Chotero iye anafesa mbewu zake, kukhulupirira Mulungu pa mgwirizano waukulu pa nyumba pa mtengo wake. Amakhalanso wothandiza kwambiri pa ntchito yomanga, choncho sanali kuopa kuigula kuti ikonzedwe.

Anatha nthawi yake kuyang’ana nyumba koma osapeza zoyenera. Koma tsiku lina akuyendetsa galimoto anaona nyumba imene inali kugulitsidwa imene anali asanaionepo. Inali yotchingidwa, ndipo pamene anali kuyang’ana, anadziwa kuti nyumbayo inali kufunika kukonzedwa, ngakhale inali kuoneka ngati inali yabwino. Anaimbira foni woyang’anira nyumbayo nkumuza kuti adzaone mtengo wa nyumbayo. Sanakhulupirire zimene anamva—madola 37,000. “Koma zingatheke bwanji?” iye anaganiza.

Woyang’anirayo adafufuza nyumbayo ndikunena nkhanu yodabwitsa. Nyumbayo inalidi yotchingidwa, ndipo idalembedwa \$110,000 pafupifupi miyezi isanu ndi umodzi mmbuyomo. Umenewo unali mtengo wa yotchingidwa, koma nyumbayo inali pa mtengo wa \$160,000 zaka zingapo mmbuyomo. Zikuoneka kuti palibe amene anasonyeza chidwi ndi nyumbayo kwa miyezi isanu ndi umodzi kuchokera pamene anaikidwa pa malonda. Kenako *nkhokwe ya ndarama* iyo inapitirizabe kutsitsa mtengowo, podziwa chifukwa chake kuti palibe amene anasonyeza chidwi. Koma pamene Tim ndi wogulitsa malo ake anafufuza mozama pang’ono, anaona chifukwa chimene panalibe chidwi panyumbayo. Inalembedwa mu mzinda wosiyana, yokhala ndi *address* yosiyanso, ndipo ngakhale nambala yafoni yofunsira inalinso yolakwika. Choncho palibe

amene anali kudziwa kuti nyumbayo inalipo! Nyumbayo, yomwe inali mumsewu waung'ono cha kunjja, pamsewu wosatuluka opanda magalimoto. Mtengo umangotsikabe mpaka tsiku lomwe Tim adazona. Zodabwitsa. Ndinauza Tim kuti nyumbayo inabisidwa chifukwa kulola iye yekha kuti agule! Anaipentanso nkuchitapo zinthu zingapo mnyumbamo nkuigulitsa pamtengo wa \$160,000.

Mwana wanga wamkazi Amy amatsogolera chipembedza ku *Faith Life Church*. Iye ndi Jason anali kufuna nyumba yaikulu chifukwa banja lawo linali kukula kuchoka pa anayi kufika pa asanu. Mitengo sinali kuoneka mu chilimwe cha 2017 kuno ku Ohio, ndipo nyumba zomwe zinali kuyikidwa pa malonda nthawi zambiri zimagulitsidwa sabata isanathe. Chiyembekezo chawo chopeza nyumba yomwe inali yaikulu mokwanira pamtengo wa \$250,000 kufika pansu pa \$300,000, yokhala ndi malo okwana maekala asanu mpaka khumi, ndi mindandanda wa zokhumba za madzi pa malowo sunapezeke. Malo odyetserako ziweto mu dera la 1 ekala amapitirira ku \$200,000 mu chilimwe chimenecho. Atathamanga kuyang'ana nyumba zambiri, anasiya kuyang'ana koma anali kupemphera. Anafesa mbewu yoti apeze njira, anauza Yehova kuti: “Ife tatanganidwa kwambiri kuona chonchi. Mumadziwa kumene nyumba yathu ili, ndipo tikukupemphani kuti mutisonyeze nyumbayo pa nthawi yoyenera. Sitidzayang'ana pa *internet*, kapena kulankhulanso ndi wogulitsa nyumba pokhudza za nyumbayi!

Koma usiku wina, chinthu chochititsa chidwi chinachitika. Mwana wawo wamkazi, yemwe anali ndi zaka zinayi panthawiyo, ananena pamene amalowa mnyumba mwawo, “Amayi, nthawi yoti musamuke yakwana. Ukutanthauza chiyani?” anafunsa Amy. “Yakwana nthawi yoti ndisamukire ku nyumba yokhala ndi masitepe aakulu amene amafika mchipinda changa,” anatero mwana wake

wazaka zinayi. “Nyumba yanji? Walota maloto?” Anafunsa Amy. Mwana wake wamkazi anati inde. Chabwino, usiku womwewo atagoneka ana awiriwo, Amy sananyoze zokambiranazo ndipo anauza Jason kuti mwina ayenera kuyang’ana pa *internet*.

Inde, inalidi yotchingidwa imene inali itangotchulidwa kumene, yosanjikizana kawiri yokhala ndi maekala khumi ndi nyanja patsogolo pake. Mtengo, komabe, unali \$26,000 kupitirira pamtengo wa \$300,000 womwe adabzala. Iwo anali kuganiza kuti nthawi zonse angapereke ndarama zochepa, choncho anaitana munthu wowagulitsira malo. Wowagulitsira anali kupita ku Florida mawa lake koma akanatha kuwaonetsa nyumbayo ngati atachita chinthu choyamba mmawa cha mma 9:00. Jason ndi Amy adanena kuti akakumana naye kumeneko.

Wowagulitsira adachedwa kutuluka kupita kunyumba, koma nyumbayo idaoneka bwino. Pamodzi ndi maonekedwe onse apanyumba, maekala khumi a malo, ndi nyanja kutsogolo, zonse zidaoneka bwino. Cholemekezetsa chinali chakuti panali nkhalango yozungulira malo onse; panali pochititsa kaso. Pamene anali kulowa mnyumbamo, mwana wawo wamkazi analira pamene anali kuthamanga kukwera masitepe akuluakulu olowera mchipinda chake. Kuti tifotokoze mwachidule, Jason ndi Amy ananena kuti amafuna kudzipereka kutchula mtengo umene angathe kupereka. Pamene wowagulitsira anayang’ana zokhudza nyumba, adapeza kuti onse amene amafuna kutchula mitengo ayenera kutero pasanafike masana tsiku limenelo. Apa ndi kuti patangokhala ola limodzi! Ngati mwana wawo wazaka zinayi sakadawauza za malotowo, ndipo akadapanda kuyang’ana pa *internet* usiku womwewo, nyumbayo bwenzi idakagulitsidwa.

Adadzipereka kutchula ndarama zokwana \$326,000 ndipo

zidatheka. Iwo anasangalala kwambiri. Panthawi yoyendera, ngakhale denga silinali looneka bwino, wowagulutsirayo adati lifunika kusinthidwa pakutha zaka zisanu kapena kuposerapo. Jason anali ndi ganizo. Anaganiza zopempha *nkhokwe ya ndarama* kuti imuchepetsere mtengo chifukwa cha denga lomwe likufunika ntchito patsogolopo. Wowagulitsirayo adawauza kuti asayese, mitengo yanyumbayo ikuperekedwa “monga momwe ilili” ndipo sanaonepo *nkhokwe ya ndarama* ikuchepetsa mtengo panyumba yotchinga chifukwa cha zolakwika mnyumbamo. Koma Jason ndi Amy anamva mumtima mwawo kulemba kalata ndikupempha *nkhokwe ya ndarama* kuti ichepetse. Mwakhoza, *nkhokwe ya ndarama* idawapatsa nyumbayo pa \$296,000, mmalo mwa \$300,000 zomwe amakhulupirira Mulungu kuti ndizo ayenera kuzigwiritsa ntchito. Mulungu anabweretsa nyumbayo monga mmene anamupemphera kuti achite. Atamufunsa woona za mitengo zomwe ana kuganiza kuti nyumbayo idakachita ndarama zingati, iye anati, “\$500,000.” Mzanga, awa ndiwo magawo kawiri!

Monga mukuonera, ana anga onse akusangalala ndi moyo wa Ufumu. Ndipotu, mwana wanga wamng’ono, Kirsten, anangolipira ndarama zogulira nyumba yake yoyamba chaka chino ali ndi zaka makumi awiri. Motani? Onse amadziwa mmene angayendetsere zimenezo mu njira ya Ufumu!

MUTU 8

MAGAWO AWIRI

Tsopano, ndikufuna kukamba mozama momwe mpumulo wa Sabata umagwirira ntchito ndi momwe zingathekere kuti ulowemo mmoyo wanu. Ndikufuna kubwereranso ku nkhani yathu ya Chaka Choliza Lipenga ndikuyang'ana palembo lathu. Pamenepo tinapeza yankho la Mulungu kwa anthu pamene anafunsa mmene akana-khalira ndi moyo wosakolola kwa zaka zitatu. Funso labwino!

Ndipo mukadzati, “Tidzadyanji mu chaka cha chisanu ndi chiwiri taonani sitidzabzala sitidzakolola zinthu?” pamenepo ndidzauza dalitso langa litsika pa inu chaka chachisanu ndi chimodzi, ndipo chidzapatsa zipatso zofikira zaka zitatu. Ndipo mubzale chaka chachisanu ndi chitatu, ndikudya zipatso zasundwe kufikira chaka cha chisanu ndi chinayi mpaka zitacha zipatso zake mudzadya zasundwe.

— Levitiko 25:20-22

Tikuona mlemboli kuti Chaka Choliza Lipenga, pamodzinso ndi chaka cha Sabata chisanafike, zonse zinali zotheka chifukwa cha zotuta zazikulu zimene zinachitika mchaka chachisanu ndi

chimodzi, pamenepa chinali chaka cha 48 (kuchokera Chaka Choliza Lipenga). Popanda kukolola kwakukulu kumeneko, mpumulo wa Sabata sukanakhala wotheke. Tiyeni tione ndime ina yomwe ndikukhulupirira imveketsa bwino za ichi.

Ndipo anauola mmawa ndi mmawa yense monga mwa njala yake, popeza likatentha dzuwa, umasungunuka. Ndipo kunali tsiku lachisanu ndi chimodzi, anaola mkati nawon-jezapo linzake—maomeri awiri pa munthu mmodzi—ndipo akazembe a khamu anadza nauza Mose. Ndipo ananena nawo: “Ichi ndi chomwe Yehova analankhula: ‘Mawa ndiko kupuma, Sabata lopatulika la Yehova. Chimene muziotcha otchani ndi chimene muziphika phikani. Ndi chotsala chikukhalireni chosungika kufikira mmawa.’”

Ndipo anausunga kufikira mmawa, monga adalamulira Mose, koma sunanunkha ndipo sunagwa mphutsi. Ndipo Mose anati, “Muudye lero, pakuti lero ndilo Sabata la Yehova; simuupeza lero pabwalo. Muziwola uwu masiku asanu ndi limodzi, koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo la Sabata; pamenepo padzakhala palibe.”

Ndipo kunali, tsiku la Sabata kuti anthu ena anatuluka kukawola, koma sanaupeze. Ndipo Yehova anati kwa Mose: “Mukana kusunga zouza zanga ndi malamulo anga kufikira liti? Taonani popeza Yehova anakupatsani Sabata; chifukwa chake tsiku lachisanu ndi chimodzi ali kupatsa inu mkate wofikira masiku awiri. Khalani yense mmalo mwake; munthu asatuluke mmalo mwake tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Ndipo anthu anapumula tsiku lachisanu ndi chiwiri.”

— Eksodo 16:21-30 (mana)

Nzoona kuti ndimeyi ikunena za mana amene anali kugwa kuchokera kumwamba tsiku lililonse kuti adyetse anthu ndipo ikufotokoza kuti sadzaonekera pa tsiku la chisanu ndi chiwiri, lomwe liri Sabata. Sakanatha kuwasunga tsiku ndi tsiku, chifukwa akanawola mofulumira kwambiri. Koma pa tsiku lachisanu ndi chimodzi lokha amawasonkhanitsa ndi kuwasunga usiku wonse popanda kuwola. Chochititsa chidwi chokhudza chifukwa chake chimene mana samawola msanga tsiku lililonse chikupezeka pa **Deuteronomo 8:16**.

Amene anakudyetsani mchipululu ndi mana, amene makolo anu sanawadziwa, kuti akuchepetseni ndikuti akuyeseni kuti akuchitireni chokoma potsiriza pano.

Mulungu anali kuphunzitsa mtunduwo kuyang'ana kwa Iye tsiku lililonse za chakudya chawo, ndithudi, komanso za chilichonse cha mmiyoyo yawo. Mulungu anali kudziwa kuti anali kufuna zinthu zambiri osati kungofuna chakudya chokha; kuti posachedwapa adzakumana ndi mizinda yokhala ndi mipanda ndi ziphona. Kudalira kwawo kokhazikika pa Iye mu mkhalidwe woterowo kukadakhala kusiyana pakati pa moyo ndi imfa.

Tiyeni tibwerere ku **Eksodo 16:29**. Pano, mukuona bwino lomwe kuti mpumulo wa Sabata unali wotheka kokha kuchokera ku magawo awiri omwe anapatsidwa kwa iwo pa tsiku lachisanu ndi chimodzi.

Taonani popeza Yehova anakupatsani Sabata; chifukwa chake tsiku lachisanu ndi chimodzi ali kupatsa inu mkate wofikira masiku awiri. Khalani yense mmalo mwake; munthu asatuluke mmalo mwake tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Kodi inu mukuziona izi? Mpumulo wa Sabata unatheka kokha ndi magawo awiri. Izi ndizofunikira kwambiri kotero kuti ndikufunsani kuti muzilembe.

MPUMULO WA PA SABATA NKOSATHEKA POPANDA MAGAWO AWIRI!

Ndiloreni ndiike mwanjira ina. Pokhapokha mutakhala ndi zochuluka, simudzakhala ndi mpumulo wakuthamangathamanga ndi kukhetsa thukuta kwa dongosolo la temberero la dziko lapansi. Monga momwe Drenda ndi ine timauzira anthu kulikonse komwe timapita, “Pokhapokha mutakonza zinthu zandarama, simudzazindikira tsogolo lanu!” Chifukwa chiyani? Chifukwa popanda kukhala ndi zokwanira koposa, simudzakhala ndi zosankha ndipo mudzakhala kapolo ku kupulumuka cha moyo wanu wonse. Kumbukirani pamene tiwerenga maphindu a Madalitso a Abrahamu kuchokera pa Deuteronomo 28:11-13 mmutu woyambirira. Kumeneko tidaona bwino lomwe kuti kukhala ndi moyo wongopulumuka si tsogolo lanu! Ngati mwaiwala, tiyeni tionenso ichi.

Ndipo Yehova adzakuchulukitsirani zokoma—mzipatso za thupi lanu, ndi mzipatso za zoweta zanu ndi mzipatso za nthaka yanu—m’dziko limene Yehova analumbilira makolo anu kuti adzakupatsani.

YYehova adzatsegula kumwamba, nkhokwe Yake ya ubwino, kugwetsa mvula pa dziko lanu mnyengo yake ndi kudalitsa ntchito zonse za manja anu. Mudzakongoletsa kwa amitundu ambiri osakongola nokha. Yehova adzakuyesani

mutu, si mchira ayi. Ngati mudzamvera malamulo a Yehova Mulungu wanu amene ndikuuzani lero ndi kuwasunga ndi kuwatsata, nthawi zonse mudzakhala wa pamwamba, osati wapansi.

— Deuteronomo 28:11-13

Umphawi, kungopulumuka, ndi kusowa ndarama si tsogolo lanu. Muyenera kukhala wongoletsa osakongola nokha, mutu osati mchira! Kuchuluka kumeneku ndi mmene Ufumuwo umaonekera. Umenewu ndiwo mpumulo wa Sabata, kukhala ndi zokwanira koposa, magawo awiri!

Ndikudziwa zomwe ukuganiza, “Ayi ndithu, zikanakhala zabwino, Gary, koma moyo wanga sukuoneka chomwecho pano.” Chabwino, sitikuyang’ana mmbuyo, koma kuyang’ana ku zomwe Mulungu akunena ndikuyembekezera zomwe Ufumu umanena za ife. Popanda chithunzithunzi cholondola, za momwe moyo wathu uyenera kukhalira, tidzagwa ku zinyengo ndi misampha ndi malingaliro opotoka a dongosolo la temberero la dziko lapansi. Chikhulupiro ndiko kukhala m’mgwirizano ndi zimene Mulungu amanena, osati ndi mmene zinthu ziliri pa moyo wathu.

Ndisanagawane nanu momwe Mulungu anaphunzitsira Drenda ndi ine za magawo awiri, ndikufuna kugawana nanu nkhani yomwe ndikukhulupirira kuti ndi nkhani yaikulu kwambiri ya magawo awiri a Chipangano Chatsopano.

Nkhani yomwe ndikufuna kugawana nanu ndi yomwe mudaimvapo nthawi

**CHIKHULUPIRO
NDIKO KUKHALA
M’MGWIRIZANO NDI
ZIMENE MULUNGU
AMANENA, OSATI
NDI MMENE ZINTHU
ZILIRI PA MOYO
WATHU.**

zambiri, koma mwina osati mu nkhani yokhudza magawo awiri kapena ndi kumvetsetsa za Ufumu umene muli nako tsopano. Timapeza nkhaniyi mu Luka 15, nkhani ya Mwana Wolowerera. Apanso, tiyeni timvere pamodzi nane. Ndikudziwa kuti mudaiwerengapo kale, koma tiyeni tionenso pamodzi ndi kuzindikira kwatsopano.

Ndipo Yesu anati: “Munthu wina anali ndi ana amuna awiri. Ndipo wamng’ono anati kwa atate wake, ‘Atate, ndigaw-irenitu zanga za pa chuma chanu.’” Ndipo iye anawagawira za pa moyo wake. Ndipo pakupita masiku owerengeka, mwana wamng’ono anasonkhanitsa zonse, napita ulendo wake ku dziko lakutali; Ndipo komweko anamwaza chuma chake ndi makhalidwe a chitaiko, ndipo pamene anatha zake zonse panakhala njala yaikulu m’dziko muja, ndipo iye anayamba kusowa. Ndipo anamuka nadziphatikiza kwa mfulu imodzi ya dziko lija, ndipo uyu anamtumiza kubusa kwake kukaweta nkhumba. Ndipo analakalaka kukhutitsa mimba yake ndi makoko amene nkhumba zimadya, ndipo palibe amene anamninkha kanthu.

Koma m’mene anakumbukira mumtima, anati, “Antchito olipidwa ambiri a atate wanga ali nacho chakudya chochuluka, ndipo ine ndionongeke kuno ndi njala! Ndidzanyamuka ndipite kwa atate wanga ndipo ndidzanena naye: ‘Atate, ndinachimwira kumwamba ndi pamaso panu. Sindiyeneranso konse kutchulidwa mwana wanu; mundiyese ine ngati mmodzi wa antchito anu.’” Ndipo iye ananyamuka nadza kwa atate wake.

Koma pakudza iye kutali, atate wake anamuona, nagwidwa chifundo; nathamanga, namkupatira pakhosi pake nampsonpsetsa. Ndipo mwanayo anati kwa iye, ‘Atate,

ndinachimwira kumwamba ndi pamaso panu. Sindiyeneranso konse kutchulidwa mwana wanu.'

Koma atateyo ananena kwa akapolo ake, 'Tulutsani msanga! Mwinjiro wokometsetsa nimumbveke. Ndipo mupatseni mphete ku dzanja lake ndi nsapato ku mapazi ake. Ndipo idzani naye mwana wa ng'ombe onenepa mumuphe. Ndipo tidye tisekere. Chifukwa mwana wanga uyu anali wakufa, ndipo akhalanso wamoyo; anali wotaika ndipo wapezedwa.' Ndipo anayamba kusekera.

Koma, mwana wake wamkulu anali kumunda. Ndipo pakubwerera iye ndi kuyandikira kunyumba, anamva kuimba ndi kuvina. Ndipo anaitana mmodzi wa anyamata namfunsa zinthu izi ndizotani. Ndipo uyu anati kwa iye, 'Mng'ono wako wafika, ndipo atate wako anapha mwana wa ng'ombe wone-nepa chifukwa anamlandira iye wamoyo.'

Koma anakwiya ndipo sanafuna kulowamo. Ndipo atate wake anatuluka namdandaulira. Koma anayankha nati kwa atate wake, 'Onani! Ine ndinakhala kapolo wanu zaka zambiri zotere ndipo sindinalakwire lamulo lanu nthawi iliyonse. Ndipo simunandipatsa ine kamodzi konse mwana wa mbuzi kuti ndisekere ndi abwenzu anga. Koma pamene anadza mwana wanu uyu wakutha zamoyo zanu ndi akazi achiw-erewere, munamuphera iye mwana wa ng'ombe wonenepa!'

Koma iye ananena naye, 'Mwana wanga, iwe uli ndi ine nthawi zonse, koma kudayenera kuti tisangalala ndi kukondw-erera, chifukwa mng'ono wako uyu adali wakufa, ndipo ali ndi moyo; anataika ndipo wapezeka.'"

— Luka 15:11-32

Mu nkhanayi tiona kuti mwana wamng'onoyo akuchoka

panyumba ndi gawo lake la chuma cha atate wake. Ichi ndi fundo yofunikira pa nkhaniyi momwe ili kulozera ku gawo lake la cholowa chake. Choncho dziwani kuti mwana wamng'ono uyu walandira kale gawo la cholowa chake; sangayembekezerenso gawo lina la chumachi.

Ndipo wamng'ono anati kwa atate wake, 'Atate, ndigawirenitu zanga za pa chuma chanu.' Ndipo iye anawagawira za pa moyo wake.

Kenako, nkhaniyi ikutiuzza kumene mwana wamng'onoyu anapita: kudziko lakutali. Ndikofunikira kuti mumvetse kuti mwana wamng'onoyu anachoka mnyumba ya atate wake, kutanthauza kuti anasiya zofunika zake, chitetezo chake, ndi malamulo a dziko limene nyumba ya atate wake inaliri. Anapita ku dziko lakutali limene linali ndi malamulo ndi njira za moyo wosiyana. Ndikukhulupirira kuti mwana wamng'ono ameneyu sanali kudziwa zimene anali kuchita. Anasangalala ndi ubwino wokhala mwana pamene anali kukhala mnyumba ya bambo ake. Zonse zimene bambo ake anali nazo zinali zopezeka kwa iye pamene anali kukhala kumeneko. Koma pazifukwa zina, iye anali kuona kuti akusowa chinachake, kumanidwa mwayi umene unali kwina kwake.

Ngati simunazindikire, kwenikweni, Yesu akutiuzza nkhanu ya anthu, nkhanu ya Adamu. Adamu ndi mwana wamng'ono wa mu nkhaniyi amene anachoka mnyumba ya Atate wake. Adamu ndi amene anaona kuti ali ndi tsogolo labwino kwina kwake kuposa kupitiriza kutumikira Mulungu, Atate wake. Ndikudziwa zomwe mukuganiza, “Chabwino, ngati Adamu ali mwana wamng'ono, wamkulu ndani mu nkhaniyi yemwe adatsalira?” Ndiyankha funsoli

kumapeto kwa kukambiranaku, koma pakadali pano, ingokumbukirani kuti Adamu ndiye mwana wamng'ono amene anachoka.

Ngakhale kuti anali ndi zonse, Adamu ndi Hava ananyengedwa kukhulupirira kuti kunali kwina kwake kumene kunali koposa kukhala mnyumba ya Atate wawo. Pamene Adamu anapandukira nyumba ya atate wake nasankha kuchoka, anakhala pansu pa boma latsopano, ufumu watsopano wokhala ndi ulamuliro watsopano, ndi malamulo oyendetsera ntchito zake. Baibulo limautcha ufumu wamdima, umene ukulamulidwa ndi Satana. Ndili wotsimikiza kuti Adamu anadabwa ndi umphawi ndi kupanda chiyembekezo kwa ufumu watsopanowu. Poyamba, zonse zinali kuoneka bwino. Ngati ndarama zake zidakhala zilipo, padakakhala phwando limodzi lalikulu! Koma pamene anazindikira kuti anakwitsa, nthawi inali itatha kale. Kenako, cholowa chake chitatha, anaona kuti wataika. Malingaliro ake, omwe kale anali odzaza ndi masomphenya, anangoima pa ntchito ya tsiku ndi tsiku yoti azingotha kukhala ndi moyo tsiku lomwelo. Sipakanakhalanso mawa. Zikadangkhalala lero ndipo lero alibe malonjezo ogwirika.

Ndipo pakupita masiku owerengeka, mwana wamng'onoyo anasonkhanitsa zonse, napita ulendo wake ku dziko lakutali; Ndipo komweko anamwaza chuma chake ndi makhalidwe a chitaiko.

Mwana wamng'onoyo tsopano akupezeka ali mu ufumu umene uli wosowa kotheratu, ufumu umene uli mu khalidwe la njala yosatha. Mwanayo akuyesera kuti agwirizane ndi zomwe akuona—anthu ali kufa ndi njala. Kuchokera ku nyumba kwa zinthu zochuluka, maganizo ake amavutika kuti aganizire zomwe

akuona. Koma ululu wa njala mmimba mwake umamukumbutsa kuti zimene amaona nzoona. Kuti apulumuke, tsopano amadzika-kamiza kupempha mmisewu. Mu ufumu wamdima uwu, dziko lapansi limangobala minga ndi mitula, ndipo kuti libale zonsezi, ntchito yowawa ndi kukhetsa thukuta iyenera kuchitidwa. Pokhala wosowa kwambiri, mwanayo akupempha wina woti amuthandize. Koma aliyense ali mngalawa imodzi. Palibe amene adzamupatse zambiri chifukwa onse akukumana ndi njala yoopsa yomwe iye ali nayonso.

Nthawi yotsimikiza ikuchitika pano kwa mwana wamwamuna, kusintha komwe kwakhudza inu ndi ine komanso anthu onse. Kwa nthawi yoyamba mmoyo wake wonse, mwana wamng'onoyo anapempha kuti alipidwe monga wantchito, wolembedwa ntchito, wochita ntchito yamanja. Uku ndi kusintha kotheratu kwa chizindikiro chake chakuti iye ndi ndani kwenikweni. Salinso mwana wa munthu wolemekezeka kwambiri waulemu ndi chuma, iye ndi wosamalira malo, kapena wogulitsa nyama, kapena wogulitsa nyumba, kapena womtuma ndi kukatenga makalata, ndipo mndandandawo ukhoza kupitirirabe. Tsopano amadziwika ndi zomwe amachita osati zomwe ali! Wataya chizindikiro chake! Kuti atsimikize kupitirira kwa chizindikiro chake, Yesu akuti adataya mtima kwambiri mpaka adapeza ntchito yodyetsa nkhumba. Nkhumba zinali kuonedwa kuti ndi zodetsedwa kwa Ayuda, ndipo Yesu akuuza khamu la anthu kuti mwana wamng'ono ameneyu tsopano wataya mtima kwambiri moti waiwala cholinga chilichonse chimene moyo wake ungakhale nacho. Panopa akukhala moyo wamanyazi ndi wonyozeka. Zaufumu zomwe kale anasangalala nazo tsopano sizikumbukiridwanso.

Ndipo anamuka nadziphatikiza kwa mfulu imodzi ya dziko lija, ndipo uyu anamtumiza kubusa kwake kukaweta nkhumba. Ndipo analakalaka kukhutitsa mimba yake ndi makoko amene nkhumba zimadya, ndipo palibe amene anamninkha kanthu.

Ndikukhulupirira kuti mukuona kufanana pakati pa nkhanayi ndi anthu lero. Amuna awiri akakumana amati chiyani? “Mumagwira ntchito yotani?” kapena “Mumagwira ntchito kuti?” kapena “Mumachita chiyani?” Mukafunsa wina kuti ndi ndani, nthawi zambiri amakuuzani zomwe amachita. Chifukwa chiyani? Chifukwa mu dongosolo la temberero la dziko lapansi, tonse tataya zizindikiro zathu (umunthu wathu), ndipo tikuyesera kuti tiupeze. Timatengera aliyense amene amakhala wodziwika ndikuoneka kuti ndi wofunikira. Zonsezi zinachokera ku chosankha cha Adamu chifukwa chochoka mnyumba ya Atate wake. Mu malingaliro athu a kupulumuka, tasiya kudziona kuti ndife ndani kwenikweni. Koma limbani mtima, mwana wamng’ono uyu mu nkhani yathu sanakhale mu khola la nkhumba; ndipo tikamatsatira nkhanayi, ndikhulupilira kuti mupeza kuti inunso simukuyenera kukhala komweko.

Baibulo limanena kuti tsiku lina mwana wamng’onyu anaganiza bwino ndikukumbukira za kunyumba ya atate wake kumene ngakhale antchito ali ndi zambiri zoti adye. Nditha kuganiza kuti ali ndi njala yaikulu, amakumbukira zakudya zabwino zonse zomwe adadya. Amalume anga Harold anali kuchita za wailesi pa B-17 mkati mwa Nkhondo Yachiwiri Yadziko lonse lapansi. Anachokera mdera la alimi komanso mu banja la alimi. Lamlungu lililonse, mayi ake anali kupereka chakudya chambiri cha nkhuu yokazinga,

mbatata yosenda, mkate wophika kunyumba, nyemba zobiriwira, ndi masamba ena okoma kwambiri. Inde, nthawi zonse pamakhala chitumbuwa chodzipangira wokha kapena keke. Ndikudziwa ndekha momwe chakudyacho chinaliri chokoma monga mayi ake anali agogo anga.

Ndege ya amalume anga inawomberedwa ku Germany panthawi ya nkhondo, ndipo anakhala miyezi yambiri mu ndende ya ku Germany. Ndipo kunalibe chakudya. Tsiku lina, ndina-funsa amalume anga mmene anapulumukira masiku amenewo, ndipo anandiuza kuti chimene anali kungoganiza chinali kupita kunyumba kukadya nkhuku yokazinga ya mayi ake ndi mbatata yosenda. Ndikukhulupirira kuti mwana wamng'ono ameneyu nayenso anakumana nazo ndipo anzindikira zimene anali kusowa. Koma analibenso gawo pa chuma chakomweko, popeza analandira kale zonse zomwe bambo ake anali nazo. Choncho anaganiza dongosolo lochita. Iye akapita kunyumba akapempha bambo ake kuti amulembe ntchito ngati wantchito.

Mu maganizo mwake, kugwira ntchito monga waganyu, inali njira yokhayo imene akadasankha.

Koma mmene anakumbukira mumtima, anati, “Antchito olipidwa ambiri a atate wanga ali nacho chakudya chochuluka, ndipo ine ndionongeke kuno ndi njala! Ndidzanyamuka ndipite kwa atate wanga ndpo ndidzanena naye: ‘Atate, ndinachimwira kumwamba ndi pamaso panu. Sindiyeneranso konse kutchulidwa mwana wanu; mundiyese ine ngati mmodzi wa antchito anu.’” Ndipo iye ananyamuka nadza kwa atate wake.

Kenako anabwerera kunyumba ndi dongosolo lake

ndikuwachonderera bambo ake kuti apeze mwayi woti agwire ntchito kuti apeze malo ogona komanso chakudya. Koma Baibulo limafotokoza mochititsa chidwi zotsatira za nkhani imeneyi. Pamene anali kuyandikira kunyumba kwake, bambo ake anamuona ali patali ndipo anathamangira kukakumana naye ndi kumukumbatira. Kuyambira pamenepo, nkhaniyo iyenera kutchedwa nkhani ya chikondi cha Atate chifukwa atatewo anamukumbatira ngakhale kuti anali kununkha ndi ndowe ya nkhumba. Mwa kuchita zimenezo, omvetsera Yesu Achiyuda anadziwa kuti kukumbatirana kudakachititsa atatewo kukhala wodetsedwa mwauzimu. Koma atate amenewa analolera kukhala wodetsedwa chifukwa cha mwana wawo. Kenako anaitanitsa mkanjo wabwino kwambiri umene anali nawo nkuuika pamwamba pa mwana wawoyo kuti aphimbe zonyansa zake. Anatenga mphete yoimira ulamuliro wake ndikuibwezeranso pa chala cha mwana wawo. Anamupatsa nsapato kuti avale, zomwe zikutanthauza kuti ali ndi mwayi wopeza chuma chonse cha moyo wawo. Koma ndi chinthu chomaliza chimene bambo ake anamupatsa chimene chimakwiitsa mwana wamkulu. Atate anaitanitsa kuti mwana wa ng'ombe wonenepa aphedwe ndi kudyedwa chifukwa chakubwera kwa mwanayo. Mwana wamng'onoyo, ngakhale kuti sanali woyenera, anapatsidwanso udindo ndi maphindu a kukhala mwana, wolemekezedwa poyera ndi mwaufulu monga mwana, ndi kubwezeretsedwa kotheratu ku malo ake akale monga mwana wa mnyumba.

Chabwino, kodi zonsezi zikukhudzana bwanji ndi magawo awiri? Chilichonse. Yesu anagwiritsa ntchito nkhani ya mwana wamng'onoyo kuchoka ndi kubweranso chifukwa omvera Ake, chikhalidwe cha Ayuda, anamvetsa tanthauzo la nkhaniyo, ndi zimene nditi ndikuuzeni. Pa chikhalidwe cha Ayuda, mwana

wamkulu ndiye amene amayenera kulandira magawo awiri. Ngati mukukumbukira, mwana wamkulu sanachoke, koma mwana wamng'onoyo ndi amene anachoka ndi kubwerera. Mudzakumbukiranso kuti pamene adachoka, adatenga gawo lachuma la malo, gawo lovomerezeka pamodzi ndi iye. Tsopano analibenso chonena pa chuma cha malo kapena chilichonse chomwe chinali mmenemo. Koma pamene mwana wamng'onoyo anabwerera atate wake anamubwezeretsa monga mwana wake, ndikumpatsanso makamaka mwana wa ng'ombe wonenepa kuti akondwerere za kubwera kwake, mwana wamkuluyo anapsa mtima. Mu malingaliro a mwana wamkuluyo, mwana wa ng'ombeyo anali wake popeza anali mbali ya gawo lake la chuma cha moyo wake.

Choncho nayi fundo yake. Ngakhale kuti wamng'onoyo anali atalandira kale gawo lake la chuma cha moyocho, anabwezeretsedwa monga mwana wamwamuna ndipo tsopano akusangalala ndi gawo lachiwiri. Izi zikadatanthauza kuti analandiradi magawo awiri a chuma cha moyo wawo. Kuchokera pamalingaliro a mchimwene wake wamkulu, ichi sichinali chilulungamo, ndipo mokwiya, amauza atate wake zomwezo. Akuti wakhala wokhulupirika kumugwirira ntchito zaka zonsezi ndipo mng'onoyu sanachite chilichonse koma kunyozetsa banja. Nanga ndi chifukwa chiani ayenera kulandira magawo awiri?

Kodi ichi chinali chilungamo? Mmaonekedwe dongosolo la temberero la dziko lapansi la zowawa ndi zokhetsa thukuta, ife tonse tinganene kuti sichinali. Tikhoza kukhala kumbali ya mwana wamkulu amene anagwira ntchito mokhulupirika ndipo akadatha kunena zopanda chilungamo pazifukwa za zimene anachitira atate wake.

Koma kodi pa chifukwa chiti chimene timaweruzza ndi

chilungamo? Kodi si atate amene amaweruza ndi kugamula kwa amene afuna kumuonetsa chisomo chake? Maphunziro a dongosolo la temberero la padziko lapansi amene tonse tikadakhala nawo angatanthauze kuti ngati atate apatsa mwana wamng'ono gawo lina lachuma cha moyo wawo, mwana wamkuluyo akadafunikira kuchita ndi zochepa. Koma izi sizili choncho. Atatewo ndi wolemera kwambiri moti ngakhale antchito ake alinso ndi zochulukira. Nanga kudakakhala bwanji kwa ana.

Satana safuna kuti mudziwe kuti Mulungu wathu ndi wamkulu kapena kuti inu ndinu ndani weniweni. Iye wakhala akufalitsa mabodza onena za Atate wathu kuyambira pachiyambi. Malamulo a *insurance* amati pamene matsoka agwa ndi kuchita kwa Mulungu. Magulu achipembedzo amanena kuti Mulungu amakondwera ndi lumbiro laumphawi. Anthu amanena kuti Mulungu amachitira zoipa anthu abwino. Satana angafune kuti mukhale akhungu kuti musazindikire kuti ndinu ndani komanso kuti Atate wanu ndi wamkulu bwanji kuti mukumbukire ndi kubwerera kwa Iye ndi mtima wanu wonse. Ndikukutsimikizirani kuti pamene mutembenukira kwa Iye, mudzapeza kulandiridwa kofanana ndi kumene kunachitikira mwana wamng'ono ameneyu mu nkhanayi.

“Mwana wamkulu ndi ndani?” inu muli kuti? Tiyeni tione ngati mungathe kuzizindikira.

Koma, mwana wake wamkulu anali kumunda. Ndipo pakubwerera iye ndi kuyandikira kunyumba, anamva kuimba ndi kuvina. Ndipo anaitana mmodzi wa anyamata namfunsa zinthu izi ndizotani. Ndipo uyu anati kwa iye, 'Mng'ono wako wafika, ndipo atate wako anapha mwana wa ng'ombe wonenepa chifukwa anamlandira iye wamoyo.'

Koma anakwiya ndipo sanafuna kulowamo. Ndipo atate wake anatuluka namdandaulira. Koma anayankha nati kwa atate wake, 'Onani! Ine ndinakhala kapolo wanu zaka zambiri zotere ndipo sindinalakwire lamulo lanu nthawi iliyonse. Ndipo simunandipatsa ine kamodzi konse mwana wa mbuzi kuti ndisekere ndi abwenzi anga. Koma pamene anadza mwana wanu uyu wakutha zamoyo zanu ndi akazi achiwewere, munamuphera iye mwana wa ng'ombe wonenepa!'

Koma iye ananena naye, 'Mwana wanga, iwe uli ndi ine nthawi zonse, koma kudayenera kuti tisangalale ndi kukondwewera, chifukwa mng'ono wako uyu adali wakufa, ndipo ali ndi moyo; anataika ndipo wapezeka.'"

Mwana wamkulu akunena kuti zaka zonsezi wakhala akutumikira atate wake, koma nthawi yonseyi, sanapatse iye kamodzi konse mwana wa mbuzi kuti asekere ndi abwenzi ake. Ndiloreni ndimasulire zomwe akunena. "Atate, mulibe chilungamo!" Koma taonani zimene atateyo akunena mobwezera.

**SATANA SAFUNA
KUTI MUDZIWE KUTI
MULUNGU WATHU
NDI WAMKULU
KAPENA KUTI
INU NDINU NDANI
WENIWENI.**

"Iwe uli ndi ine nthawi zonse, ndipo ZONSE ZIMENE NDIRI NAZO ndi zako."

Imani!!!!

Tsopano, kodi mungadziwe kuti mwana wamkulu ndi ndani? Mwana wamkulu wakhala wotanganidwa kwambiri kutumikira atate wake ndi maganizo olakwika kudzilungamitsa kuti asangalale ndi ubwino wa atate wake.

Chilichonse chomwe atate ali nacho ndi chake nthawi yonseyi.

Mukunena zoon, mwana wamkulu akuimira lamulo la pangano loyamba. Mwana woyambayo sakanatha kusangalala ndi maphindu a nyumba ya atate wake chifukwa chakuti anali wotanganidwa kwambiri ndi ntchito kuti atate wake avomereze. Ngakhale kuti mwana wamkulu anali ndi ufulu wolandira magawo awiri, pamenepa anali mwana wamng'ono yekha amene anasangalala nawo.

Ndiwe mwana wamng'ono!

Muli ndi magawo awiri. Ndiwe mwana wolandiridwa osatengera zomwe umachita koma kutengera momwe ulili mwa Kristu—mwana wamwamuna kapena wamkazi wa Mulungu, wolandira cholowa chomwe sunachigwirire ntchito koma kuchilandira kwaulere kwa Atate wako.

MUTU 9

KUKHALA NDI ZOKWANIRA KOPOSA!

Ndikumvetsa kuti mungakhale mukukaikira phunziro la mutu uno, koma kumeneku ndi kumene mukupita, kukhala ndi zokwanira koposa. Osati chifukwa chakuti ndikukuonetsani dongosolo laposachedwa kwambiri lopangira ndarama koma chifukwa monga mwana wa Mulungu ndi ufulu wanu wovomerezeka kusangalala ndi zabwino ndi zotukuka za nyumba ya Atate wanu. Lingaliro la magawo awiri, kukhala ndi zokwanira koposa, limatha kuoneka ngati zosatheka kulingaliridwa pompano poyerekeza ndi komwe mumadzionera nokha pakali pano mmoyo wanu. Koma ndi pamene muyenera kuyamba ulendo wanu wopita ku ufulu—mu maganizo anu. Pokhapokha ngati malingaliro anu akugwirizana ndi Mawu a Mulungu, simudzasangalala ndi maphindu Ake. Tsono kwezani maso anu kuchoka ku zimene muona ndi kuyang’ana pa zimene Mulungu akuti ndi zanu mu ufumu Wake. Lekani kutsutsana ndi zomwe Mulungu akunena chifukwa simukuziona mmoyo wanu. Mmallo mwake, yambani kutsutsana ndi zochitika zanu ndi Mawu a Mulungu, kukhulupirira kuti ayenera kugwirizana kuti zonse

zomwe Mulungu amanena ndi zanu. Ine ndine munthu ngati inu amene ndinangochita zimene ndikukuuzani kuti muchite. Khulupirirani zomwe Mulungu akunena! Mawu a Mulungu sangalephere

**LINGALIRO LA MAGAWO
AWIRI, KUKHALA NDI
ZOKWANIRA KOPOSA,
LIMATHA KUONEKA
NGATI ZOSATHEKA
KULINGALIRIDWA
POMPANO POYEREKEZA
NDI KOMWE
MUMADZIONERA NOKHA
PAKALI PANO MMOYO
WANU. KOMA NDI
PAMENE MUYENERA
KUYAMBA ULENDO WANU
WOPITA KU UFULU—MU
MAGANIZO ANU.**

ndipo adzabweretsa kusintha kwa mkhalidwe uliwonse. Mwachitsanzo, iyi ndi *email* yomwe ndilandira kuchokera kwa womvera yemwe amakaikira, adamva zonse, kapena adazimvadi?

“Ndidzayesera kuika zaka makumi awiri ndi mphambu ziwiri zovuta mmawu ochepa mothekera.” Ine ndi mwamuna wanga tinakulira mu mabanja a Chikristu ndipo tinali kupita kutchalitchi nthawi zonse. Tinali kuchita nawo chinyamata, Sande sukulu, ndi zina zotero. Pamene tinakwatirana, chaka chathu choyamba pa zachuma zinali zabwino ... zinali zaka makumi awiri ndi mphambu ziwiri zapitazo. Chiyambireni nthawiyo, “ndarama”zo zinali magwero a

zowawa ndi zovutirapo nthawi zonse, ndipo chikhulupiriro changa chinali kugwedezeka nthawi zonse chifukwa sindinali kumvetsetsa chifukwa chimene Malembo amanena chimene chiyenera kuchitika koma sichinachitike. Ngati Mawu a Mulungu anali amuyaya ndi osavunda ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawi zonse,

ndiye amapereka chiyani? Mwina anali wofera chikhulupiro, wabodza, kapena wamisala!

“Posachedwa pa January 28, 2013 ... Ndinauza mwamuna wanga, 'Mwina Mulungu aonekere kapena ndichoke.'” ... Ndinali nditasiya mpingo ndi Mulungu. Pamene ndinachoka mnyumbamo kukachita ntchito zingapo, mwamuna wanga pomalizira pake anamva chilimbikitso cha Mzimu Woyera ndipo anaitana mnzanga wapamtima kuti tikambirane. Atamaliza, anena kuti ali ndi chinachake choti timvetsera, Gary Keese. Adapereka umboni wake pazomwe zidamuchitikira. Choncho, nditafika kunyumba mwamuna wanga anandiuza zimene ananena ndipo anali kupita tsiku lotsatira kuti akazitenge.

“Sindikudziwa zomwe zinachitika” (chifukwa ndinamva zokwanira kwa abusa ndi aphunzitsi za “zinthu zauzimu” zonse), koma ndinamuitana, ndikumufunsa ngati analipo madzulo amenewo. Pakati pausiku wa *snow* wambiri, ndinafika kunyumba kwake. Pamene ndinali kuyendetsa galimoto, ndinauza Mulungu kuti, 'Zikadakhala bwino zitero!'

“Tsiku lotsatira, tinayamba kumvetsera, ndipo tonse awiri tinathedwa nzeru. Zonse zinayamba kukhala zomveka.” Ndime zonsezo: chikhulupiro, kugwiritsitsa chivomerezo chatu. Zosamvetsetseka zonse zidakhala mmalo mwake. Tinali titamva za Ufumu zaka zingapo zapitazo, KOMA palibe amene anakhala ndi chidwi chophunzitsa NJIRA zake ... monga mungafikire pamalo oti 'NDI IZI!' Inu munatero.

“Choncho nthawi yomweyo, tidagwiritsa ntchito zomwe tadaphunzira” ... timafuna ndarama zolipirira nyumba yathu. Linali Lachinayi, ndipo mwamuna wanga anali atamaliza ntchito zina

zing'onozing'ono kunyumba kwa makolo anga... anandifunsa kuti amupatse ndarama zingati mwamuna wanga (anadziwa kuti zinthu zinali zovuta). Ndinawauza kuti, 'Chilichonse chimene akufuna.' Sizinali zokwanira kulipira ngongole ya nyumba ... KOMA linalidi Lachinayi lokha.

“Lachisanu, tinakonza zoti tikakumane ndi mnzathu amene anatibwereketsa ma *CD*.” Kunagwa *snow* yambiri, koma ine ndi mwamuna wanga tinafuna kukhala pansu ndi kulankhula naye za Ufumu ndi mmene unagwirira ntchito.

“Tisananyamuke, anafuna kupemphera, ndipo anatipatsa cheke ... chimene Ambuye analimbikitsa pa mtima wake kuti afese mmiyoyo yathu.” Chimenechi chinatithetsa mphamvu. Kenako tidatsegula cheke...chinali CHOKWANIRA KOPOSA kulipira ngongole yanyumba ndi zina za zing'onozing'ono!

“Ndinauza mwamuna wanga kuti izi ndizo zonse zomwe ndimafuna!” Ndinajambula cheke kuti chindikumbutse za kukhulupirika Kwake. Chabwino, mdani sanakonde zomwe adazona ndipo nthawi yomweyo (ndipo inu, ndikutanthauza nthawi yomweyo!!!!) adayesa kuba mbewu yathu. Tinali kuganiza kuti zimenezi zinali zoonza, ndipo sitinalankhule chilichonse chimene chidakawononga tsogolo lathu. Anali wosatopa ... koma tidakhazikika ndikuimiritisa chishango chathu.

“(Tsopano ndisanapitirire, ndikufuna kuti mumvetse kuti ndinali Mtaliyana wouma mutu amene ndinatopa ndi 'ziphunzitso za kutukuka' zomwe ndinamva ... mwamuna wanga anadziwa ichi.)” Chozizwitsa choona chinali chakuti ndachigwiritsitsa ndi kuchikangamira ... nthawi zina mwamuna wanga amandiyang'ana ndikudabwa chomwe chinachitika!

“Tinamasula chikhulupiriro chathu ndi kufesa kuti tilandire

contract ya *company* yathu yomanga pa 3/13 ya *contract* ya \$150,000 yoti tilipire ngongole zosalipidwa, misonkho, ndi zina zotero!!!!” Pa April 5/13, tinalandiranso ma *contract* awiri okwana \$450,000 TSIKU LIMODZI!!!! Izi zinali patangotha miyezi iwiri kuchokera pamene tinayamba kugwiritsa ntchito fundo za Ufumu.

“Tinalowetsamo ana athu kuti achite nawo ndipo anaona kuti ’ndi izi.” Tsopano, adzipangira okha mndandanda ndi kufesa mu nkhoekwe zawo za *nkhokwe ya ndarama* ya nkhumba kubzala zimene akufuna. Tili ndi gawo mu chipinda chilichonse, ndipo mwana wathu wazaka zisanu amapita kwa iwo nkunena kuti, ‘Ndikukhulupirira kuti ichi ndachilandira.’

“Tili oyamikira kwambiri kuti tsopano tili ndi ndarama zambiri zoti tipereke ndiponso kuti latsala tsiku limodzi loti tisakhale ndi ngongole kuti tikwanitse ntchito yathu!”

“Zikomo, Mbusa Gary, chifukwa chopatula nthawi kuyankha ma *email* omwe ndanakutumizirani. Tikudziwa kuti mulibe nthawi yokwanira, ndipo kuti munapatula nthawi yochitira zimenezi zikusonyeza mmene mukufunira kuuza ena uthenga wodabwitsa wa Ufumu waukulu wa Mulungu umenewu.”

Ndimalandila ma *email* ngati awa tsiku lililonse. Anthu onga inu ndi ine tikupeza choonadi ponena za amene ali mwa Kristu, akuphunzira mmene Ufumu wa Mulungu umagwirira ntchito, ndi kusangalala ndi maphindu ake. Tsono kodi ine ndi Drenda tinazindikira bwanji fundo ya magawo awiri? Ndikuuzani mmutu uno ndipo ndikudziwa kuti mudzapeza nkhani zathu zili zolimbikitsa.

Ine ndi Drenda tinayamba kuphunzira malamulo ndi fundo za Ufumu wa Mulungu, miyoyo yathu inasinthidwa kwambiri, monga ndinakuuzani mu chigawo choyamba cha buku lino, tinali kukhala ndi ndarama zochepa, kulimbana ndi vuto la mantha, mankhwala

oletsa kupsinjika mmaganizo, ndiponso kosowa chiyembekezo ku moyo wa cholinga ndi zofunikira. Tinaona zinthu zikuchitika mobwerezabwereza zimene zinapangitsa ife kuima ndi kunena kuti, “Mwaona izo? O-oo!” Tinaona Ufumu wa Mulungu ukugwira ntchito monga momwe Baibulo linanenera, ndipo tinafunsa mafunso, “Kodi zimenezo zinachitika motani kapena chifukwa chiyani?” Kapena “Kodi tinatsatira fundo yotani?” Ngakhale kuti tinali kusangalala kwambiri, sitinaone magawo awiri momveka bwino monga nkhani zimene nditi ndikusonyezeni.

Tinasangalala ndi magawo awiri, komabe, sitinadziwe kutchula zomwe tinaona kuti ndi magawo awiri mpaka Mulungu adachulutsa kumvetsetsa kwathu. Ndisanafotokoze momwe Mulungu anatithandizira pakumvetsetsa magawo awiri mopitirira, ndikufuna kubwereza Lembo lathu lofunikiranso kwa mphindi imodzi. (Mawu omwe ali mu *mabacket* ndi anga, osati gawo la Lembo lenileni.)

Momwemo utatsalira mpumulo wa Sabata wa kwa anthu a Mulungu. Pakuti iye amene adalowa mpumulo wake, [chikhulupiriro] adapumulanso mwini wake ku ntchito zake [dongosolo la temberero la dziko lapansi ndi ntchito zowawa, kukhetsa thukuta, ndi kupulumuka], monganso Mulungu ku zake za Iye.

— Aheberi 4:9-10

Pakali pano mukudziwa kuti mpumulo wa Sabata uwu ndi lonjezo kwa wokhulupirira aliyense wa Chipangano Chatsopano mwa Kristu ndipo sichinthu cha Chipangano Chakale chabe. Mukudziwanso tsopano kuti Sabata silingatheke popanda kukhala ndi zokwanira koposa, kapena monga tinaonera

mu Eksodo 16, magawo awiri. Chonde musasokoneze kuti poyenda mu magawo awiri kutanthauza kuti nthawi zonse mudzakhala ndi ndarama zambiri zotsalira pamene Mulungu akufunsani kuti muyambitse zochitachita.

Pali nthawi zina mmoyo wanga pamene Yesu anandiuza kuti ndipite patsogolo ndi zochitachita zimene ndinalibe ndarama ku nkhoekwe ya ndarama. Kenako ndinazindikira kuti Mulungu analibe nkhwawa ndi ndaramazo ndipo anali kudziwa kumene zidzachokera. Koma sadalole kuti zionekere, kuopera mdani kuti angayese kuziba zisanafunike. Ndiloreni ndikuchenjezeni, ingotsimikizani kuti mupite patsogolo mu chinthu chonga chimenecho ngati muli otsimikiza kuti mwamva kuchokera kwa Mzimu Woyera kuti mutero. Apanso, pokhapokha Yesu atakuuzani kuti mupite patsogolo ndi zochitachita popanda ndarama, musachite. Dikirani mpaka nthawi ya Mulungu ndi zofunikira zake kuti zipezeke.

Mwambiri, ife monga okhulupirira timaitanidwa kuti tikhale ndi moyo wakusefukira kwa chuma mmiyoyo yathu. Sitili aumphawi koma okhoza pakuwolowa manja nthawi zonse monga momwe Atate wathu alili. Ndimangotchula izi chifukwa ndalandira ma *email* ambiri omwe anthu anasiya ndikuphonya nthawi ya Mulungu. Mvetserani, chifukwa chakuti Mulungu wakusonyezani china chake sizitanthauza kuti yafika nthawi yoti muchichita. Nthawi zambiri, amakuonetsani china chake chokupatsani njira komanso nthawi yokonzekera. Mwachidziwitso changa, nthawi ndi yofunikira kwambiri monga momwe kuli kofunikira kumvera malangizo.

Yesu atayamba utumiki wake mmudzi wa kwawo, atabatizidwa mu mtsinje wa Yorodano ndi Yohane Mbatizi ndipo patapita masiku makumi anayi, usana ndi usiku mchipululu, analowa mu sunagoge ya kwawo ndi kutenga mpukutu wa buku la Yesaya ndikutsegula

mutu wa makumi asanu ndi limodzi ndi chimodzi ndikuwerenga. Tikupeza chochitika ichi cholembedwa pa Luka 4:18-21.

Mzimu wa Ambuye uli pa ine, chifukwa chake Iye anandidzoza ine ndiuze anthu osauka uthenga wabwino. Anandituma ine kukalalikira a m'nsinga mamasulidwe ndi akhungu kuti apenyenso, kutulutsa ndi ufulu wopwanyika, kukalalikira chaka chosankhika cha Ambuye.

Ndipo mmene Iye anapinda Bukulo, nalipereka kwa mnyamata, anakhala pansi. Ndipo maso awo a anthu onse msunagogemo anamuyang'anitsa Iye, ndipo anayamba kunena kwa iwo, kuti, "Lero lembo ili lakwanitsidwa mmakutu anu."

Zoonadi, iwo anakwiira Iye posonyeza kuti ndiye amene anali kunenedwa. Koma tcherani khutu pamene Yesu anasiya kuwerenga. Ndime yoyamba mpaka yachiwiri ya Yesaya 61 imati,

Iye wanditumiza ndikamange osweka mtima, ndikalalikire kwa a m'nsinga mamasulidwe ndi kwa omangidwa kutsegulidwa kwa mndende, ndikalalikire chaka chokomera Yehova ndi tsiku la kubwezera la Mulungu wathu.

Onani kuti Yesu anaima pakati pa fundo. Iye sanawerenge, "ndi tsiku la kubwezera la Mulungu wathu." Chifukwa chiyani? Chifukwa anafuna kuima pa gawo loyamba ya fundoyo, "chaka chokomera Yehova." Kodi chaka chokomera Yehova ndi chiyani? Chaka Choliza Lipenga!

Yesu anali kulengeza kwenikweni kuti zonse zimene mthunzi wa Tsiku la Sabata, Chaka cha Sabata, ndi Chaka Choliza Lipenga zinationetsa kuti zakwaniritsidwa ndipo tsopano lino ndi chifukwa

chake Iye anabwera. Mutu wonse wa Yesaya 61 umatiuza zimene Yesu watichitira. Pankhani ya magawo awiri, onani ndime 7 mpaka 9.

Mmalo mwa manyazi anu owirikiza ndi chitonzo iwo adzakondwera gawo lawo; chifukwa chake iwo adzakhala nacho mdziko mwawo cholowa chowirikiza, adzakhala nacho chikondwerero chosatha. Pakuti Ine, Yehova ndikonda chiweruziro; Ndida chifwamba ndi choipa. Ndipo ndidzawapatsa mphotho yawo mzoonadi ndipo ndidzapangana nawo pangano losatha. Ndipo ana awo adzadziwika mwa amitundu ndiobadwa awo mwa anthu. Onse amene awaona adzawazindikira kuti iwo ndiwo ana amene Yehova wadalitsa.

— Yesaya 61:7-9

Ndikumvetsetsa ndikamachita manyazi chifukwa mavuto azachuma ogwetsa ulesi. Nthawi zambiri ndinali kudziona ndikunzozedwa, ndikuchita manyazi chifukwa cha mavuto athu azachuma. Ndikukumbukira nthawi ina ndinasonkhanitsa anzathu pafupifupi makumi awiri kudzadya ku malo odyera a kwathuko. Sindikukumbukira unali mwambo wapadera otani umene tinali kuchita, koma ine sindinalipire zonse. Ndikumbukira kuti ndinavutika pa mwambowu chifukwa ndinalibe ndarama zolipirira. Ndarama zimene

**CHIFUKWA
CHAKUTI MULUNGU
WAKUSONYEZANI CHINA
CHAKE SIZITANTHAUZA
KUTI YAFIKA NTHAWI
YOTI MUCHICHITA.
NTHAWI ZAMBIRI,
AMAKUONETSANI CHINA
CHAKE CHOKUPATSANI
NJIRA KOMANSO
NTHAWI YOKONZEKERA.**

ndimayembekezera za malonda amene ndinachita zinachedwa kufika. Khadi lotengera ndarama linali litatsekedwa ndipo linali litadetsedwa osadziwa kuti likhoza kugwira ntchitonso. Potsirizira kuti ndilipire, khadilo linakanidwa. Ndipo modzichepetsa ndinafunsa mmodzi mwa oitanidwa anga kuti alipirire mwambowo.

O-oo, ndili ndi nkhani zambiri ngati zimenezo, koma sindikutsimikiza kuti muli ndi mphamvu yokwanira kuti muyambe kuchita zotere. Koma alemekezeke Mulungu, kudzera mwa Yesu, onse amene amationa adzayenera kuvomereza kuti ndife anthu amene Yehova watidalitsa!

Magawo awiri ndi anu, Yesu ndiye mpumulo wanu wa Sabata, ndipo Iye ndiye magawo anu awiri! Ngati munawerengapo lililonse la mabuku anga akale, mukudziwa kuti Ambuye anandiphunzitsa zambiri za Ufumu kudzera mkusaka agwape. Chenicheni, kusaka agwape inali galimoto imene Mulungu anagwiritsira ntchito kukopa chidwi changa choyamba cha Ufumu. Ndinakhala ndikusaka agwape kwa zaka zingapo koma sizinaphule kanthu. Ngakhale kuti ndinali kuikapo nthawi ndi ndarama zanga, sindinapeze chipambano kapena kupeza nyama. Kunena zooni sindinaomberepo. Chaka chimene ndinali kuganiza za nyengo imene inali kubwera yosaka agwape, Mulungu analankhula nane nati, “Bwanji osandilola kuti ndikuthandize ndi kusaka agwape chaka chino?” Zachidziwikire, sindimadziwa zomwe izi zinali kutanthauza, koma adandiuza kuti nditenge cheke ndikulemba kuti, “Gwape wanga wa 1987” pagawo la zikumbutso, pamodzi ndi ndarama zina, ndikuzitumiza ku utumiki kumene Iye anandiuza kuti nditumizire. Anandiuzanso kuti ndikhale ndi Drenda ndikusanjika manja athu pa cheke chime-necho ndi kugwira mawu a pa Maliko 11:24 pamene tinapemphera icho.

Maliko 11:24 akuti,

Chifukwa chake ndinena ndi inu, zinthu zilizonse mukazipemphera ndi kuzipempha, khulupirirani kuti mwazilandira, ndipo mudzakhala nazo.

Kuti ndifotokoze mwachidule, ndinapita kumalo osadziwika bwino chaka chimenecho ndipo ndinagwira gwape wanga patangotha pafupifupi mphindi makumi anayi. Drenda ndi ine takhala tikutsatira izi kwa zaka makumi atatu apitawo, ndipo ndakhala ndikukulola agwape anga pakati pa mphindi makumi atatu mpaka anayi chaka chilichonse kuyambira pamenepo. Mzaka zonsezi, ndaona Mulungu akuchita zinthu zodabwitsa kwambiri posaka agwape, ndipo ndaphunzira zambiri zokhudza malamulo a Ufumu kudzera mkusakasaka. (Nkhani zonse zoyambirirazo zinalembedwa mu buku langa lakuti *Faith Hunt*.)

Nthawi zambiri ndimakonda kusaka mnyengo ya chilimwe kenako mnyengo yozizira kuno ku Ohio. Chiwerengero cha agwape amene mungasake ndi chabwino ndithu, ndipo mchaka chilichonse, malire a agwape amene ndimapeza pa chaka ndi asanu ndi mmodzi. Sindinasakepo kusaka agwape ochuluka chotere kuti ndidyetse banja langa. Mu firiji mwanga nthawi zambiri mumakhala modzaza ndi agwape awiri kapena atatu pachaka. Kuti munyadire zomwe ndikufuna kukuuzani, muyenera kudziwa kuti pamene ndinali kusaka zaka zonsezi ndinali ndisanawomberepo agwape awiri pamtengo womwewo pa kusaka kwa mmawa kapena kusaka kwa madzulo. Mwa njira imeneyi, ngati simuli mlenje, inde, timasaka kuchokera pamtengo. Nthawi zambiri, pamene ndikupha gwape, ndimachoka mu nkhalango ndikubweranso tsiku lina

ndikudzaphanso wina. Koma Ambuye anali kufuna kundiphunzitsa china chake pa kusaka kwamadzulo uku.

Linali limodzi mwa masiku abwino kwambiri osaka kutha kwa chilimwe, kunali mitambo pang'ono ndi kamvula kanali kugwa nthawi ndi nthawi. Linali Lamlungu madzulo, ndinali wotopa pang'ono chifukwa chochititsa misonkhano ingapo mmawa umenewo, ndipo ndinali kuyembekezera kukakhala mu nkhalango. Drenda anali kupita kokagula zinthu zingapo, ndipo ine ndi iye tidagwirizana kuti uwu ukhala usiku wabwino kuika nyama mu frigi. Ndinavala chovala change chodzibisa ndikusonkhanitsa zinthu zanga pamene amatuluka kupita ku galimoto. Ndidatuluka panja pamene amanyamuka. Pamene amayendetsa galimoto, adatsitsa zenera ndikundiiza kuti, “Magawo awiri.” Sindinadziwe chifukwa chake ananena zimenezo, ngakhale pambuyo pake ananena kuti anamva Ambuye akunena zimenezo kwa iye panthawiyo ndipo analimbikitsidwa kundiuza zimenezo.

Tinapha agwape atatu chaka chimenecho, ndipo ili linali tsiku loyamba kukasaka nyengo imeneyo. Ndidamupsopsona mwachangu ndikumuuza kuti ndavomera, ndipo ndidanyamuka kupita kunkhalango kwathu. Ndimasaka pamalo panga, choncho ndinali kudziwa bwino kumene ndinali kulowera. Nditakwera pamtengo wanga, ndinakuwa kangapo moita agwape. Mkati mwa mphindi khumi ndi zisanu, wamkulu wa nyanga za nsonga zisanu ndi zitanu anabwera akuthamanga, ndinamuombera motalikira mayadi makumi anayi, ndipo anagwa pansu. Zimenezo zinali zodabwitsa! Ndinatsika ndikupita kwa gwape, koma kenako ndinakumbukira zomwe Drenda adanena, magawo awiri, koteru ndinasiya gwape pomwe adagwera ndikubwerera kumtengo wanga ndikukweranso pamalo paja.

Ndidaganiza ndi chipwirikiti chomwe ndidachita potsika, poyenda mozungulira, kenako pobwerera pamalopo ndikukwera, komanso fungo lomwe ndidabalalitsa pochita zonsezi, kuti mwachilengedwe zikadabweretsa mwayi wochepe wakupha wina mu mphindi zochepe zotsala za kuwala kovomerezeka mwalamulo posaka. Koma pasanathe mphindi khumi ndi zisanu ndili mumtengowo, kamwana ka gwape kadaenda pansu pa mtengo wanga, ndipo ndinamupha mwakumuwombera bwinobwino. Inde, kuwombera kawiri ndikupha agwape awiri motsatana kuchokera mumtengo womwewo. Ndinali ndisanachitepo zimenezi. Ichi chidandigwira mtima ndipo ndidadziwa kuti ndi magawo awiri omwe Drenda adalankhula.

Kwa zaka zisanu zotsatira, ndinakumana ndi chinthu chofanana. Nthawi zonse ndikapita kokasaka ndi uta, ndimapeza agwape awiri kuchokera mumtengo womwewo mwa mphindi zosiyana. Ndinadziwa kuti zimenezi sizinali monga mwachikhalidwe, ndipo ndinayamba kukhazikika pamagawo awiri, kudziwa kuti Mulungu amatiphunzitsanso phunziro lina la Ufumu Wake.

Nthawi zonse ndimakonda mfuti, ndithudi, ndimakonda kusaka. Ndili ndi mfuti zanga zomwe ndimagwiritsa ntchito posaka, ndipo ndinali wokondwa kwambiri ndi mfuti zomwe ndinali nazo. Ine ndi Drenda tili ndi malo okwana maekala makumi asanu ndi limodzi ndi maekala pafupifupi makumi awiri ndi asanu a nkhalango ndi maekala ena khumi ndi asanu a madambo. Mu nthawi ina yakuyamba dzinja, madambo akhoza kukhala ouma kapena odzaza madzi, malingana ndi mmene chilimwe chinaliri.

Chaka chomwechi, tinali ndi chilimwe chamvula kwambiri, kotero kuti madambowo anali odzaza ndi madzi pamene nyengo ya dzinja la abakha inafika. Nthawi zonse kudali abakha akubwera

mmadambo chaka chilichonse kumene madzi anali, koma sindi-nawalabadire kwenikweni. Koma chaka chino kunali abakha akuluakulu amene anali kubwera mmadambo kumene madzi anali ochuluka kwambiri, ndipo sindidathe kuwaletsa. Ngakhale kuti sindidayambe ndawasaka mmbuyomo, ndinaganiza kuti ndipite ku madambo kukayesa kusaka abakha. Chabwino, kusakaku kunali kwakukulu. Panali abakha paliponse, ndipo tinali ndi chakudya chamadzulo cha abakha chaka chimenecho.

Posaka abakha chaka chimenecho, ndinaona kuti nthawi zambiri abakha anali kungodutsa kutali. Ndinali kugwiritsa ntchito mfuti yanga tsiku ndi tsiku, yomwe nthawi zambiri ndimagwiritsira ntchito posaka akalulu ndi mbalame, koma pamene abakha anawuluka patali ndi mfuti, ndinakumbukira kuti ndinamva za mfuti zatsopano zomwe zinapangidwira kusaka abakha. Izo zinali zobisika ndipo zimadatha kuwombera abakha ambiri kwa nthawi yaitali. Ndimakumbukira kuti ndimayenera kukaziyang'ana nthawi ina.

Eya, zidangochitika kuti ndinali musitolo yogulitsa za masewera mdera lathu, mwezi umodzi itatha kwa nyengo ya abakha pamene ndidaona gulu la mfuti zolembedwa kuti mfuti za mbalame. Ndinaziyang'ana pang'ono, zinali pamtengo wa \$2,000 ndipo fundo yakuti ndikadadikira miyezi khumi osaigwiritsa ntchito ndikuyembekezera nyengo ina ya abakha, ndinaganiza kudikira mtengo wotsika. Koma mosaganizira, ndinati, “Ambuye, ndingakonde kukhala ndi iyo.” Sindinaganizire kwambiri za izo pamene ndinali kuchoka musitolo, koma masabata angapo pambuyo pake ndinali kulankhula pamsonkhano wamalonda wa *macompany*, osati msonkhano wa tchalitchi. Kumapeto kwa kulankhula kwanga, *CEO* adandithokoza chifukwa cholankhula ndipo adati,

“Tikufuna kukuthokozani ndi mphatso chifukwa cholankhula usiku uno.” Ndinachita mantha pamene anatulutsa mfuti imene ndinaiyang’ana musitolo yogulitsira zinthu zamasewera milungu ingapo mmbuyomo. Mawu anga akuti, “Ambuye, ndingakonde kukhala ndi iyo,” ndiponso fundo yakuti ndinali nditapereka mfuti mmbuyomo tsopano zinabweretsa zokololazo.

Mu buku loyamba la mndandanda uno, *Kusinthika Kwa Chuma Chanu: Mphamvu ya Kukhulupirika*, ndikukamba za fundo yomwe inachititsa kuti mfutiyo ioneke. Ndimachitcha kuti fundo ya zenga, ndipo ikupezeka pa Maliko 4:26-29. Ndikupangira kuti mupeze kope la bukulo ngati simudaliwerenge kale. Mfuti yomwe ndidaionayo inali yodabwitsa kwambiri, koma si nkhani yeniyeni yomwe ndikufuna kuyang’anapo. Koma idayambitsa nkhani yomwe ndikufuna kukuuzani.

Nditaona mfutiyo, ndidazindikira momwe ndidayambira kukolola, tsiku lina ndidalingalira kwa mphindi zingapo za mfuti ina iliyonse yomwe ndinaganiza kuti ndikanakhala nayo. Ndipotu, ndinali nditafesa mfuti zambiri, choncho ndinaganiza kuti ndiyese- setse kutsatira malamulo a Ufumu. Mfuti yokha yomwe ndinalibe mgulu la mfuti zanga inali mfuti yowombera patali ndi pafupi (*over and under shot*.) Ndi mfuti zokongola, ndipo nthawi zambiri sizitsika mtengo. Kotero ine ndinati, “Ambuye, ine ndikanafuna nditakhala ndi imodzi ya zabwino izo, mfuti zowombera patali ndi pafupi!”

Patapita pafupifupi mwezi umodzi, ndinalandira foni kuchokera kwa mnzanga wina wa muutumiki, ndipo anandiuzza kuti akufuna kundigulira mfuti yamphamvu kwambiri. Ndinasangalala kwambiri ndipo ananena kuti aitumiza. Eya, patapita masiku angapo ndinalandira mfuti ziwiri zokongola, zokongola kwambiri! Onani kuti

ndinalandira mfuti ziwiri. “Inde,” ndinaganiza. Ndinamuimbira foni mnzangayo ndi kumuthokoza chifukwa cha mfuti zokongola zimene anatumiza. Mmasiku angapo otsatira anatumiza zinanso awiri. Nditamuimbiranso kuti ndimuthokoze, ananenanso kuti: “Ndinachita chidwi kwambiri kuti munandiimbira foni kuti mundithokoze, ndipo ndinafuna kukutumizirani zina ziwiri.” Ine ndinali okondwa kwambiri ndi mphatso, koma ndinali ndikuyamba kuona kufanana pamenepa. Mfuti ziwiri nthawi iliyonse? Zikumveka ngati magawo awiri.

Pafupifupi miyezi iwiri yapitayo, ndinali kuphunzitsa patchalitchi china mmawa ndipo ndinayenera kukaphunzitsa mumzinda womwewo pa tchalitchi china usiku umenewo. Utumiki wa mmawa utatha, mwamuna wina anabwera kwa ine nkunena kuti, “Ndikutumizira mfuti yokongola ya *Browning semiautomatic* yomwe ndili nayo.” Apanso ndinasangalala kwambiri. Chodabwitsa ndi chakuti, pa msonkhano wamadzulo wa kutchalitchi china, mwamuna wina anabwera ndi kunena kuti: “Ndabweretsa mfuti yatsopano imene idakali mu bokosi imene ndikufuna kukupatsani.” Inali yokongola, yojambulidwa ndi Marlin 30/30, mfuti yomwe nthawi zambiri ndimaisilira koma sindinakhale nayo. Apanso, ndinadabwa koma ndinali nditagwira—magawo awiri.

Komanso, patapita masabata angapo, chinthu chomwecho chinachitika—mfuti ziwiri zinapatsidwa kwa ine tsiku limodzi. Chabwino, zomwe ndinganene ndikuti ndine munthu wodalitsika ndi mfuti zazikulu ndithudi. Koma monga nkhani iliyonse yomwe ndimafotokoza, nthawi zonse ndimafunsa kuti, “Zinachitika bwanji?” Inde, ndakuuzani kale kuti ndabzalapo mfuti zambiri mmbuyomu koma sindinanene kuti, “Ambuye, ndingakonde kukhala ndi iyo,” mpaka pamenepo. Apanso, iyi ndiye fundo ya

zenga yomwe muyenera kuyidziwa. Koma popitirira fundo ya zenga, ndinali kulowa m'magawo awiriwa mwaluso komanso momveka bwino ndipo ndinali kufuna kudziwa momwe ndinali kuchitira. Ndikhulupirira kuti Ambuye anandisonyeza kuti ambiri a ife taphonya mbali yofunika kwambiri imeneyi ya kututa kuchokera ku Ufumu, ndipo nditenga nthawi ina mmutu wotsatira kufotokoza phunziro lake. Koma ndisanatero, ndikungokuuzani momwe chaka chimenecho chinapitirizira kutha kwake.

Nditalandira mfuti, nkhani iyi inachitika—ndipo ndi imodzi mwa nkhani zodabwitsa kwambiri zomwe zakhala zikuchitika poona magawo awiri akuonekera momveka bwino, popanda mafunso omwe amafunsidwa, ichi ndi chitsanzo cha magawo awiri. Nkhaniyi ikukhudzana ndi magalimoto anga, makamaka *Cadillac Escalade* ya ngale yoyera yomwe idapatsidwa kwa ine imene ndidatchulapo mitu ingapo yapitayo. Monga ndidanenera kale mu bukuli, mtima wanga ndi wa Drenda suli pamagalimoto. Nthawi zambiri timangowayendetsa mpaka atasiya kugwira ntchito kapena osaoneka bwino.

Ndiponso mu nkhanayi, ndiyenera kunena kuti Drenda ndi ine tidaperekapo magalimoto angapo mmbuyomo ndipo sitinafotokoze momveka bwino za chikhulupiriro chathu pazomwe timakhulupirira kuti tidzakolola kuchokera ku kupereka kumeneko. Koma ngati mukukumbukira nkhani imeneyo, pamene tinali kuyendetsa galimoto yobwerekera *Escalade* pamsonkhano wathu ndi kunena kuti, “Timakonda iyi; tikuganiza kuti tikhale ndi imodzi mwa izi,” sitinali kuyembekezera kuti wina atiimbira foni ndikunena kuti akufuna kutigulira. Komatu ndi zimene zinachitika. Ndipo, ndithudi, sitinauze aliyense kuti tinafuna imodzi yotere. Chifukwa chake monga ndidakuuzani kale, yamtundu wa ngale yoyera,

Escalade yaifupi idaoneka bwino kwambiri. Ndimaikonda.

Koma pali mbali ina yochititsa chidwi kwambiri pa nkhani imeneyi imene inachitika mchilimwe chathachi. Tinali titayendetsa *Escalade* iyi kwa pafupifupi chaka ndi theka koyambirira kwa chilimwe chatha, ndipo tsiku lina ndinazindikira za kuyaka

NDIKUTSATA

MFUMU NDI UFUMU

WAKE, KOMA MU

UFUMU NDIMAPEZA

ZOKWANIRA KOPOSA,

MAGAWO AWIRI!

kochenjeza zomwe zimachitika ku injini. “Palibe vuto lalikulu,” ndinaganiza, koma ndinali kufuna kuti ndifufuze, kotero ndinafuna wodziwa kuti aione. Iwo ananena kuti si nkhani yaikulu ayi. *Sensor* inapereka chenjezo mafuta pang’ono *exhaust*, koma sizingayambitse vuto. Injiniyo idzakhale choncho nthawi yonse imene ndidzi-

yendetsa. Ndinawafunsa chifukwa chake chimene inali kupereka chenjezoli. *Escalade* yanga inali ndi *exhaust* imene inaikidwa itaguludwa kale, ndipo iwo anaganiza kuti icho chikhoza kukhala chifukwa chomwe kuyakaku kunaonekera. Apanso, adanena kuti injiniyo inali yabwino ndipo ndiyenera kuyembekezera kuti injiniyo idzakhala nthawi yaitali.

Tsiku lina, pochezerana ndi bambo amene anandipatsa galimotoyo, ndinatchula vuto la kuyaka kwa *sensor* yomwe ndinali nayo. Anati, “Inde, ndaonapo izi zikuchitika ndi magalimoto ena a GMC.” “Ndipotu,” iye anatero, “zimachitika ku magalimoto akale.” Anapitiriza kunena kuti sizingaononge galimotoyo mwanjira iliyonse ndipo ndikhoza kuyendetsa galimotoyo kwa zaka khumi kapena kuposerapo popanda vuto.

Anadziwa kuti ine ndi Drenda tili ndi nyumba ku Florida yomwe ndinali nditangogula kumene. Ndinakhala modabwa pamene anati,

“Ndikuuzeni. Inu muyendetse iyi ku Florida ndi kukaigwiritsa ntchito kumeneko, ndipo ine ndikugulirani yoti muziyendetsa kuno ku Ohio.” Inde, tsopano ndili ndi zangale yoyera ziwiri, ma*Escalade* aafupi omwe anali abwinobwino mwanjira iliyonse, kupatula kuyaka kwa *sensor* komwe kumabwera kamodzi pakanthawi. Onse ali bwinobwino mu njira iliyonse! Apanso, iyo inali imodzi mwa izo, “Kodi inu munazona izo?” zosaiwalika. Ine ndi Drenda tiyenera kudzitsina tokha pamene tikuyendetsa magalimoto okongola amenewo. Sitinalipire ngakhale imodzi mwa magalimoto amenewo. Koma mu nkhani iyi, tinadziwa kuti anali magawo awiri.

Sindikunena nkhani izi kudzitamandira mwanjira iliyonse, koma mnzanga, ndine wodala! Ndikusangalala ndi magawo awiri, monga momwe mukudziwira, kukhala ndi zokwanira kuposa. Ndili ndi chosungira mfuti ndipo ndi chodzaza ndi mfuti, zomwe ndizokwanira koposa. Ndili ndi ma *Escalade* awiri ofanana omwe sindinalipire. Ndikuganiza kuti mungavomereze kuti izi ndi zokwanira koposa! Ndipo sikuti ndikukulimbikitsani kuti muzifunafuna zinthu zakuthupi, ayi. Ndimapatsidwa zinthu momasuka, ndipo sindipembedza zinthu kapena kuzitsata. Ndikutsata Mfumu ndi Ufumu Wake, koma mu Ufumu ndimapeza zokwanira koposa, magawo awiri!

Dikirani, sindinathe kuchitira umboni za ubwino wa Yehova ndi magawo awiri pakali pano.

Mkazi wanga anali kufuna nyumba ya mu mphepete mwa nyanja kwa zaka makumi awiri zapitazi. Ayi, ndiloreni ine ndifotokozenso izo. Akhala akufuna kwamuyaya! Amakonda nyanja! Komabe, akhala akuyang’ana nyumba ku nyanja kwa zaka zambiri. Mmbuyomu pamene panali mwayi wogula nyumba imene anali kuikonda, ndarama zathu zinali zitapatulidwa kale ku ntchito za

utumiki ndipo tinali kungoyembekezera. Chabwino, chaka chino ndinali kupemphera mchipinda chapansi pamene ndinali kuchita monga za masiku onse. Mwadzidzidzi, Ambuye anakoma mtima kwambiri, “Kauze Drenda kuti apite ku Florida, tauni yomwe akufuna kukhalako ndi nyumba, ndipo umuuzza kuti agule nyumba yake yapafupi ndi nyanja sabata ino.” Eya, sabata ino? Panali changu champhamvu mu mzimu wanga nditamva izi. Choncho ndinamuuzza Drenda zimene Ambuye anandiuza, ndipo tinalumikizana ndi mnzathu amene anali kukhala mumzindawo kuti tione ngati angafune kumuyendetsa Drenda kwa masiku angapo kuti akaone nyumba. Anati angakonde kutero.

Chifukwa chake Drenda adapita pa *internet* ndikupanga mndandanda wanyumba pafupifupi makumi awiri mphambu zisanu zomwe amafuna kuziona. Atafika kumeneko, Drenda adachepetsa mndandanda wa nyumba makumi awiri mphambu zisanu kufika pa zisanu zofunidwa kuphatikiza ndi imodzi imene amati amaikonda. Pa nthawiyi, ndidapita ndi ndege kukamana naye ndipo adandionetsa nyumba zisanu ndi yomwe anakonda. Tinachepetsa zisanu kufika pa ziwiri—zomwe anali kuzikonda ndi nyumba ina yomwe inali yabwino kwambiri koma yosaoneka bwino ngati imene anali kuikonda. Ndinavomereza nditaona nyumba yomwe anali kuikonda, ndinadziwa kuti ndi Drenda, ndipo pomaliza tinaikapo mtengo wathu wogulira. Mwini wakeyo anavomera mtengo wathu ndipo tinalowa mpanganano lakukhala ndi nyumba yathu yatsopano.

Patatha milungu ingapo, pamene tili kwathu ku Ohio tikupumula, Drenda anadzuma ndi kunena kuti, “Iyi ndi nyumba yanga!” “Ndikudziwa,” ndinati, “Iyi ndi nyumba yako. Mulungu anandiuza kuti ndiyenera kukugulira nyumba yako ya kunyanja pamlungu umene ndinakutumiza kunyanja.”

“Ayi,” iye anatero, “simukumvetsa; ndiyo nyumba yanga.” Iye anapitiriza kufotokoza kuti wakhala akufunafuna nyumba kwa zaka zingapo mu dera limenelo, ndipo tsiku lina anaona chithunzi cha nyumba imene tinali kugula pa malonda a malo ogulitsa nyumba. Ataona, anaikonda. Iye anali kukonda chilichonse za iyo, mamangidwe a chi*Spanish Mediterranean*, dongosolo lapansi, malo, chilichonse. Anakumbukira kuti anaika chala chake pachithunzichi ndi kunena kuti, “Ambuye, ndikufuna nyumba imeneyo!” Koma anali kudziwa kuti nyumbayo ndi yodula kwambiri ndipo tinali titapereka kale ndarama zathu kuzinthu zina, choncho anali kungoyang’ana nyumba zomwe zinali pamitengo yathu panthawiyo. Koma palibe nyumba ina yomwe inaganiziridwa, ndipo sitidafike pa fundo yeniyeni yoika pangano pa imodzi. Tinalibe mtendere pa zokhudza nyumba.

Muyeneranso kudziwa kuti tidabzala mbewu ya nyumba ya mumphepete mwa nyanja mu tauniyi zaka ziwiri zapitazo. Chivomerezo chathu panthawiyi chinali chakuti tili ndi nyumba ya mu mphepete mwa nyanja mu tauni ino, tili nayo kale, ndipo tinailandira tsiku limene tinaifesa. Ndikukumbukira malo enieni komanso mphindi yomwe tidagwirana manja ndikuvomerezana za malo a nyumba ya kunyanja ya Drenda. Koma tsopano pamene tinali m’pangano, Drenda mwadzidzidzi anakumbukira chithunzi chimene anaona zaka ziwiri zapitazo ndipo anazindikira kuti iyi inali nyumba yomweyo, nyumba yake!

Titafufuza mbiri ya nyumbayo, tidapeza kuti mwini nyumbayo adayesadi kugulitsa nyumbayo zaka zingapo zapitazo, koma siinagulidwe ndipo adaichotsa pamsika wa malonda. Pamene ndi pamene Drenda adaona chithunzi cha nyumbayo pamndandanda wake wanyumba zogulitsidwa. Ndipo mwini wakeyo anali ataikanso,

ndipo izi zikufotokoza chifukwa chake ndinafulumira kutumiza Drenda kunyanja ndi malangizo akuti, “Mudzagula nyumba sabata lino.” Adzakuuzani kuti si mmene ndimawonongera ndarama, nthawi ndi chilichonse. Panthawiyi, ndarama zanga sizinali za ntchito zina koma zinalipo zogulira nyumba. Ndikukhulupirira kuti panali anthu ambiri omwe anali kuyang’ana nyumbayo ndipo chinali chifukwa chake chakuchitira changu. Chodabwitsa ndi chakuti mtengowo unali usanakwere pamtengo umene unalembedwa zaka ziwiri mmbuyomo pamene anauona koyamba. Ine ndikukhulupirira Mulungu anali kumusungira iye!

Koma pamenepa pali magawo awiri a nkhanayi. Pamene nyumba yathu inali m’pangano kudikira kutsekedwa, tinalandira foni kuchokera kwa mayi ake a Drenda. Iwo anali ndi nyumba ku Canada kwa zaka makumi atatu ndi mphambu ziwiri zapitazi. Tinalipo kumeneko kangapo kwa zaka zambiri ndipo tinali kukonda nyumbayo komanso malowo. Nyumbayo ili pachilumba. Ndipotu, Nyanja yake ili pafupi ma *feet* makumi atatu kuchokera kumtunda wakumbuyo. Makolo a Drenda anali atakalamba ndipo adaganiza kuti sakufuna kusamalira ndi kumwaza ndarama pa nyumba kuti zichuluke. Anabwera kwa ife natifunsa ngati tinali ndi chidwi chogula ndipo ndinakana. Unali ulendo wa maola makumi atatu ndi limodzi kuchokera ku Ohio, ndipo ngakhale kuti ndinali kukonda malowa, sindinali kuwaona kuti ndi chinthu chimene ndidakatha kufikako nthawi zambiri chifukwa cha nthawi yapaulendo. Chifukwa chake adalembetsa nyumbayo kwa wogulitsa malo, koma atakhala nayo pamsika kwa zaka ziwiri, palibe wogula yemwe adaonetsa chidwi chachikulu.

Chotero tsopano pamene tinali kuyembekezera kusiya za nyumba yathu ya mu mphepete mwa nyanja, anatiimbira foni

ndi kulongosola kuti anayesa kugulitsa nyumbayo koma popanda amene anaifuna. Tinali ndi ndarama zokwanira theka ngati tifuina kugula ndi kusungiramo banja. Pamene ndinaganizira chimenezi, ana anga anali atakula akupita kumeneko ndipo ndi malo abwino kwambiri. Choncho ine ndi Drenda tinapempherera nkhaniyi ndipo tinati kuti agule. Tinali ndi ndarama zimene zinalipo kuti tigule. Kuwonjezera apo, tinali titagulira ndege ya *company* yanga chaka chopita, zimene zinatilola kukafika kumeneko mu maola asanu mmalo mwa maola makumi atatu ndi limodzi amene anali kufunika pagalimoto. Izi zinapangitsa kupita kumeneko mosavuta kwambiri.

Titagula nyumba zonse ziwiri, tsiku lina nditakhala mu ofesi yanga, mwadzidzidzi ndinamva kuti, “Tadikira mwa mphindi, awa ndi magawo awiri!” Mkazi wanga wakhala akulota za nyumba ya kunyanja mwa zaka zambiri. Tsopano, mmiyezi iwiri, anapeza nyumba yomwe ili kummwera kwa United States, yomwe imakhala yotentha mnyengo yozizira koma yotentha kwambiri moti sangathe kuigwiritsa ntchito mchilimwe. Koma nyumba yaku Canada ndiyabwino mchilimwe koma imazizira kwambiri mnyengo yachisanu. Tinazindikira kuti tsopano ali ndi nyumba ya kunyanja ya nyengo zonse ziwiri. Zodabwitsa. Tidati, “Kodi mwaona?” pamene kugula kuwiri kuja kunatenga malo. Ndikuganiza kuti mungavomereze kuti izi zikuoneka komanso zikugwirika ngati magawo awiri! Zodabwitsa!

**NDIKUFUNA
KUONETSETSA KUTI
SIMUKUGANIZA KUTI
MAGAWO AWIRIWA
AMAKHALA NDI
ZINTHU ZIWIRI
ZOKHA. KWENIKWENI,
MAGAWO AWIRIWA
NDI KUKHALA NDI
ZOKWANIRA ZOPOSA.**

Ndagwiritsa ntchito zitsanzo zingapo za momwe Mulungu anabweretsera ziwiri za china chake kwa ine ndi Drenda, zomwe ndimakhulupirira kuti Mulungu anali kugwiritsa ntchito kuti tione bwinobwino magawo awiri akugwira ntchito. Koma ndikufuna kuonetsetsa kuti simukuganiza kuti magawo awiriwa amakhala ndi zinthu ziwiri zokha. Kwenikweni, magawo awiriwa ndi kukhala ndi zokwanira zoposa. Mulungu anali kugwiritsa ntchito zitsanzo zosiyana kwambiri za ziwiri za china chake kuti chikope chidwi changa za magawo awiri. Kaya ndi zotani, kukhala nazo zochuluka ndizo magawo awiri. Ine ndikuyembekeza inu mukugwira chenicheni cha magawo awiri ndi mpumulo wa Sabata. Umoyo ndi wodabwitsa kwambiri mu Ufumu! Pamene ndikulemba mutu uwu, ndikukhala mnyumba mwathu ku Canada, ndikuyang'ana pa zenera kunyanja. Mu mphepete mwa nyanja muli timbalame takunyanja ndi abakha omwe akusewera mayadi 25 okha kuchokera ku nyumba yathu. Kuli mtendere, palibe kukanika, zolipiridwa, ndi madalitso. Ndili pa ntchito, kugawana mbiri yabwino ya Ufumu wa Atate wanga, mwana mnyumba Yake, nzika ya Ufumu Wake waukulu, ndipo ndikusangalala ndi magawo awiri!

Ine ndi Drenda titha kulemba nkhani zambiri za momwe Ufumu wa Mulungu ndi malamulo omwe amaulamulira zikhudza miyoyo yathu, komanso zikwi za anthu omwe amatitumizira ma *email* ndi nkhani zawo. Monga ndinafotokozerana, mungawerenge zinthu zonsezi mu Baibulo, koma ndi zosangalatsa kwambiri kuona Baibulo likufotokozedwa pamaso panu.

Pali chapadera chomwe ndikufuna kuwonjezera apa. Ndivuto lalikulu kwa ine kuuza anthu momwe Mulungu wadalitsira ine ndi Drenda komanso ulendo womwe tayenda. Anthu nthawi zambiri amalakwitsa. Nthawi zina angaganize kuti ndife onyada kapena

odzitamandira. Kapena akuganiza kuti tatenga chakhumi chawo kapena zopereka zawo kuti tiwadyere. Chonde mvetsetsani kuti ine ndi Drenda sititenga ndarama pa TV yathu, ndipo sititenga ndarama pakugulitsa za chuma chathu. Inde, timapeza malipiro, ndithudi, kuchokera ku tchalitchi chimene timatumikira. Koma tili ndi malonda athu ndipo ndi athu nthawi zonse ndipo Mulungu amawadalitsa. Ndikungofuna kutsimikiza kuti mudziwe mitima yathu pogawana nanu nkhanu zathu. Ndinaona kuti ndiyenera kukuuzani zimene taona zikuchitika, ndiponso zimene Mulungu watiphunzitsa pa zochitika zimenezo. Zotsatira zomwe ndikugawana nanu sizotsatira za Gary ndi Drenda Keese; sitiri abwino chotero! Ayi, zimene taona ndiponso zimene tikusangalala nazo ndi zotsatira za Atate wathu ndi Ufumu wake mmiyoyo yathu. Timagawana nanu nkhanu chifukwa tikungofuna kuti mumve! Inde, tinalibe chilichonse ndiye ndi chifukwa chake ndikulembera bukuli kwa inu! Ndikufuna kuti mudziwe momwe zimagwirira ntchito kuti mumvetsetse ndikulandira zonse zomwe Mulungu ali nazo kuti ndi za inunso.

Mvetsetsani kuti ndimadana ndi umphawi ndi mtima wonse. Zaka zisanu ndi zinayi zimenezo za kukhala mu kupsinjika maganizo kosalekeza ndi mantha zinali ngati kukhala ku gehena wadziko lapansi, kwenikweni! Ndikukhulupirira kuti mudzakumbukira kuti mpumulo wa Sabata ndi wanu komanso wanga! Mu mutu wotsatira, ndidzakuthandizani kuti mumvetsetse mmene mungalowere mu mpumulo wa Sabata.

Fundo yapadera chabe ya mutu uno. Nditangomaliza kulemba chiganizo pamwambapa, mlembi wanga adalowa muofesi yanga nandiuza kuti bokosi lafika la ine. Ndinadabwa ndikutsegula ndipo ndinapeza mfuti ziwiri zabwino kwambiri. Inde, zinali zolimbikitsa!

Zinali ngati kuti Mulungu akuika “Amen” pa zimene ndinali nditangonena kumene.

Bukuli litapita kukasindikizidwa ndipo nditalandira mabuku oyamba pokhala ndi galimoto, ndinali wokondwa kuphunzitsa fundozi kwa nthawi yoyamba pamsonkhano wathu wa *Revolution* ya Atlanta. Ndinasangalalanso kukhala ndi buku langa latsopano kuti ndikapatse anthu. Ndikukonzekera kupita kuchipinda chochezera kuti ndikalankhule, mlembi wanga adandiimbira foni ndikundiiza kuti pali foni yochokera kwa mwamuna yemwe adandipatsa mfuti zoyamba, ndipo adati akufuna kulankhulana nane. Ndinamuiimbira foni. Iye anasangalala kwambiri pamene anafotokoza kuti iye anapita ku ofesi ya *UPS* ndipo ananditumizira mfuti zina ziwiri! Kupatula apo, akadatumiziranso mfuti ya Drenda, ndipo podziwa kuti sasaka, adamutumizira \$1,500 pazolipira za zana limodzi. Ndinadabwa kwambiri. Ndinaona kuti anali Mulungu akutsimikiziranso zimene ndinali kuchita ndipo, mwanjira ina, akundiiza kuti ndipitirize. Anthu ayenera kudziwa izi—Mulungu akufuna kuti mudziwe izi! Komabe, nditafika kunyumba, ndinali wokondwa kutsegula bokosilo. Drenda ndi ine tidalandira mfuti zokongola kwambiri za Browning zomwe ndidazionapo. Zonse zinali zatsopano. Ndinalinso ndi *Browning gold semiautomatic 20 gauge* ndiponso, Drenda anali ndi \$1,500. Magawo awiri!

Mwina mwake mukudabwa chifukwa chiani ndili ndi mfuti zambiri. Chabwino, ndiyenera kuvomereza kuti tsopano ndili ndi mfuti zabwino kwambiri, osati zotsika mtengo, ndipo ndidafunsanso funso lomwelo. Mulungu adandidziwitsa kuti adatumiza mfuti zodula kwambiri komanso zokongola kuti andionetse momwe chuma Chake chinaliri, kuti zofunikira Zake kwa ife ndi zopitilira zomwe ndinkayembekezera ngakhale kupitilirapo. Ndikumvetsetsa! Ndikuona!

MUTU 10

CHINSINSI CHA MAGAWO AWIRI

Tsopano ndafotokoza kuti mpumulo wa Sabata ndi chiyani ndi mmene zimathekera kudzera mu magawo awiri. Funso lomwe liyenera kukhala mmaganizo mwanu ndilakuti, “Kodi ndingapeze bwanji magawo awiri?” Chabwino, ndakondwa kuti mwafunsa! Kuti tipeze yankho la funsoli, tiyeni tibwererenso ku nkhani imene Yesu anadyetsa amuna zikwi zisanu ndi mikate isanu ndi nsomba ziwiri.

Ndipo pamene dzuwa linapendeka, anadza kwa Iye ophunzira ake nanena, “Malo ano ngachipululu, ndi dzuwa lapendeka ndithu. Muwauze kuti amuke alowe kumilaga ndi midzi yozungulira akadzigulire okha kanthu kakudya.”

Koma iye anayankha nati kwaiwo, “Apatсени kudya ndinu.”

Ndipo iwo ananena naye, “Imeneyo ingatenge ndarama yoposa miyezi isanu ndi itatu ya malipiro! Kodi tingapite ife ndikukagula mikate ya pa malupiya a theka mazana awiri ndikuwapatsa kudya?”

Ndipo Iye ananena nawo kuti, “Muli nayo mikate ingati?” Anafunsa. “Pitani mukaone.”

Ndipo pamene adadziwa ananena, “Isanu—ndi nsomba ziwiri.”

Ndipo anawalamulira kuti anthu akhale pansi onse mmagulumagulu pa msipu. Ndipo anakhala pansi mabungwe mabungwe a makumi khumi ndi a makumi asanu. Ndipo Iye anatenga mikate isanuyo ndi nsomba ziwirizo, nayang’ana kumwamba, nadalitsa, nagawa mikate; napatsa ophunzira kuti apereke kwa iwo. Ndi nsomba ziwiri anagawira onsewo. Ndipo anadya iwo onsewo nakhuta. Ndipo anatola makombo, mitanga khumi ndi iwiri, ndiponso za nsomba. Ndipo amene anadya mikate iwo anali amuna zikwi zisanu.

— Maliko 6:35-44

Tidakambirana kale za nkhaniyi, koma pali zowunikira zazikulu pano za magawo awiri. Mu nkhaniyi, Yesu mwauzimu

**ILIPO NJIRA YABWINO
YOKHALIRA NDI MOYO KUPOSA
KUNGOFUNA KUKHALA OKHUTIRA.
SIMUNGATHE KUMANGA
ZAMBIRI NDI MALINGALIRO
OKHUTITSIDWA. MASOMPHENYA
SAYANG’ANE KUTALI POKHALA
PA MLINGO WOKHUTITSIDWA
WONGOYANG’ANA ZA LERO LOKHA.**

anachulukitsa mikate ndi nsomba, ndipo anthu anadya kufikira kukhuta. Ndikuganiza kuti panali anthu pafupifupi 20,000, kuphatikiza akazi ndi ana; ndi kuti anthu ambiri anadyetsedwa ndi mikate isanu ndi nsomba ziwiri, kufikira aliyense atakhuta, ndicho chotsimikizirika cha Mulungu. Ndipo chifukwa cha zimenezo,

tikhoza kukondwerera za Ufumu ndi mmene unagwirira ntchito. Koma kungodyetsa anthu sichithunzithunzi chonse cha zimene zinachitika, kungoimira pamenepo ndiye musiya magawo awiri. Tiyeni tifufuze pang’ono.

Ndipo anadya iwo onsewo nakhuta. Ndipo anatola makombo, mitanga khumi ndi iwiri, ndiponso za nsomba. Ndipo amene anadya mikate iwo anali amuna zikwi zisanu.

Kotero lembo lilikutiuzwa chiyani? Kuti onse atakhuta, mitanga khumi ndi iwiri yodzala ndi mikate ndi nsomba inatoledwa. Tanthauzo la magawo awiri ndikukhala ndi zokwanira koposa. Kukhala wokwanira ndiko kukhala wokhutitsidwa, koma mitanga khumi ndi iwiri yotsala anthu atakhuta ndiyo magawo awiri, zokwanira koposa. Chonde lolani kusiyana kumeneko kukhazikike mu chikumbumtima chanu pang’ono. Ndikufuna kuti mukhale ndi chithunzithunzi chomveka bwino cha ndime ya kukhutitsidwa ponena za magawo awiri mu malingaliro anu. Ndilibenanthawi pano kuti ndifotokoze mozama mmene Yesu anabweretsera mphamvu ya Ufumu mu mkhalidwe umenewo kuti akwaniritse mbali yoyamba ya nkhanayi—anthu zikwi zisanu anakhutitsidwa. Koma mutha kupeza kufotokoza kokwanira mu buku loyamba la nkhanizi, lotchedwa *Kusinthika kwa Chuma Chanu: Mphamvu ya Kukhulupirika*.

Mmalo mwake, ndikufuna kuyang’ana pa magawo awiri, kusefukira, ndi momwe zinachitikira mu nkhanayi. Inde, ndi nkhanu yodabwitsa—anthu 20,000 onse anakhutitsidwa, Inde! Koma zilipo zambiri mu Ufumu kuposa kungokhutitsidwa, ngakhale kuti mufunikiradi kukhala okhutitsidwa musanapitirire

ku kusefukira. Kukhala wokhutitsidwa ndikwabwino, kodi za mawa bwanji? Chomwe ndikuyesera kunena ndichakuti ngati cholinga chanu ndikungokhuta, chimachitika ndi chiyani mukamvanso njala? Akristu ambiri ali mu mkhalidwe lokhala atakhutitsidwa koma amaphonya magawo awiri. Ndi magawo awiri omwe amabw-eretsa mpumulo wa Sabata la Mulungu. Kukhala wokhutitsidwa ndi kwa kanthawi kochepe. Sikuthetsa vuto la zofunikira. Kudziwa kuti mudzakhalanso ndi njala ngakhale simuli ndi njala tsopano kumatsegulabe khomo la mantha, zomwe zimakupangitsani kuthamangathamanga ndikugwira ntchito ndi malingaliro ofuna kupulumuka. Ayi, ilipo njira yabwino yokhalira ndi moyo kuposa kungofuna kukhala okhutira. Simungathe kumanga zambiri ndi malingaliro okhutitsidwa. Masomphenya sayang'ane kutali pokhala pa mlingo wokhutitsidwa wongoyang'ana za lero lokha. Kungokhala wokhutitsidwa ndi cholinga chakupulumuka ku moyo padziko lapansi mu machitidwe a dongosolo la temberero la ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta.

Kukhutitsidwa kumadya za lero; magawo awiri amamanga za mawa!

Ndiloreni ndikupatseni chitsanzo cha momwe chikhalidwe ndi mipingo yambiri imaganizira. Funsani aliyense momwe akuchitira pa zachuma ndipo mudzapeza mayankho ambiri, mwina osati ambiri abwino. Koma ngati mupeza abwino, wina akuti, “Tikuchita bwino,” mufunseni, “Kodi munatenga nthawi yaitali bwanji kuti mulipire nyumba yanu?” Iwo mwina angakuyang'aneni ndi kunena, “Chabwino, nyumba yanga siinathe kulipidwa. Ndinali kungotanthauza kuti tikulipira ngongole zathu zonse ndipo tili ndi ndarama

kunkhokwe yathuyandarama.” “Chabwino!” inu mukuti, “Anyamata inu mukuchita bwino. Ndiuzeni, kodi muli ndi ndarama zoposa \$10,000 kunkhokwe ya ndarama?” Zachidziwikire, palibe amene angafunse izi, ndikuganiza, ngati mukadatero akadayankha kuti, “Ayi, koma tili ndi \$800.” Kunena zoon, anthuwa akuganiza kuti akuchita bwino pa zachuma chifukwa ali ndi galimoto yabwino, nyumba yabwino, ndi ndarama zocheza kunkhokwe ya ndarama. Akukhala moyo wokhutitsidwa. Koma zilipo zinanso! Nanga bwanji kuti nyumba yanu ilipidwe ndi \$100,000 kunkhokwe ya ndarama, kapena \$500,000 kunkhokwe ya ndarama? Chimenecho chingakhale chithunzithunzi chokwanira koposa cha moyo kwa anthu ambiri. Kukhutitsidwa ndikwabwino komanso kofunikira, koma kukhala ndi madengu khumi ndi awiri a mkate ndi nsomba mu chipinda mosungira chakudya ndi kokwanira koposa, ndipo pamakhala mtendere!

Ndinakhala pansu ndi wamalonda tsiku lina ndikukambirana naye za chuma chake. Pamene ndinali kuona ngongole zake, ndinaona kuti anali ndi ngongole pafupifupi \$40,000 ya m'makhadi a ngongole. Ndipo pamene ndinali kuona katundu amene anali naye, ndinaona kuti anali ndi ndarama zokwana \$40,000 mu *checking account*. “Joe,” ndidati, “izi ndizopanda nzeru. Uli ndi ndarama zoti ulipire makhadi ako a ngongole atatu kotheratu. Chiwongola dzanja chako pa makhadi a ngongole ndi 18%, ndipo chiwongola dzanja pa *checking account* yako ndi 1%. Lipira makhadi a ngongole! Koma kodi mukudziwa chiyani? Joe adati sakufuna kutero. Ndinakhala pamenepo ndikudabwa, ndipo ndinamufunsa chifukwa chake. Iye ananena kuti kukhala ndi ndaramazo mu *checking account* yake kunamupangitsa kukhala wotchinjirizidwa komanso wolemera. Ndinangomuyang'ana. “Ukutanthauza chiyani

kuti umadziona ngati wolemera? Ichi ndi chinyengo. Ngakhale uli ndi \$40,000 mu *checking account* yako, ulibe \$40,000 chifukwa uli ndi ngongole ku *macompany* a makhadi a ngongole ya \$40,000. Malingaliro ako ndi abodza, ndipo ukulipira ndarama zambiri kuti ukhulupirire chinyengocho.”

Tinakambitsana kwa pafupifupi ola limodzi, ndipo sanathe kumvetsa chifukwa chimene anayenera kulingalira ndi za kuika ndarama zambiri mu *checking account* yake monga inalili ngongoleyo, zimene anandikumbutsa kuti anazigwirira ntchito molimbika. Ndinagonja patatha ola limodzi lina ndikubwerera kunyumba. Iye ananyengedwa; analibe chitetezo poyesa kusunga ndaramazo mu *checking account* yake. O-oo, ndikudziwa kuti zidaoneka bwino pamene lipoti la ndarama idabwera m'makalata likuonetsa kuti \$40,000 ili ku nkhekwe ya ndarama. Koma kuti akhale ndi chithunzithunzi choti adziwe kumene iye anali, anafunika kutsegulanso makhadi a ngongole.

Kukhutitsidwa ndi kwabwino, ndipo kukhoza kukukopani mu malingaliro abodza a chitetezo. Muyenera kuyang'ana kumbuyo pang'ono ndikudziwa kuti zomwe mwangodya sizingathe kukupatsani zomwe mukufuna mu maola angapo. Mudzakhalanso ndi njala. Ngati mukuyang'ana kuchita kofulumira, kukhutitsidwa mofulumira ku zofunikira, kudzakuphonyetsani chinthu chokhacho chimene kwenikweni chikhoza kusintha moyo wanu—magawo awiri.

Pamene ife tonse tinakulira mu dongosolo la temberero la dziko lapansi la zachuma la ntchito zowawa ndi zokhetsa thukuta, tinalota za chinthu chimodzi, kusiya! Ndinatchula izi mu mutu wapitawu. Sitinaganizire za ntchito yowonjezereka kapena mwayi wina chifukwa, kunena zoonza, tinali otanganidwa kale ndi za umoyo ndipo tidangodikira kuchita kwina. Mukuona, akapolo salota za

ntchito yambiri. Akapolo amalota chinthu chimodzi—Lachisanu usiku, osati Lolemba mmawa. Chifukwa chiyani? Chifukwa akapolo amalota chinthu chimodzi chokha—kuima. Mvetserani, otanganidwa ndipo “sakhoza kudikira kuti aime” malingaliro anu sangakufikitseni kulikonse. Ngakhale mngelo atalowa mchipinda chanu ndikukuuzani lingaliro lochokera kwa Mulungu, malingaliro anu angakulepheretsenibe. Lembani izi.

MUYENERA KUONA KUBZOLA KUKHALA WOKHUTITSIDWA KUTI MUGWIRE MAGAWO AWIRI!

Mawu awa ndiye chinsinsi cha magawo awiri. Ndikudziwa kuti sizikupanga nzeru pakali pano, koma zidzatero. Kutu ndikusonyezeni zimene ndikutanthauza, ndikufuna tionenso nkhani ya kudyetsa anthu zikwi zisanu mu buku la Yohane, mmalo mwa buku la Maliko. Malinga ndi mmene Yohane anali kuonera nkhaniyi, timapezanso nkhani imodzimidziyo koma ndi fundo zochepa zimene sitizipeza mu Buku la Maliko.

Pamenepo Yesu anatenga mikateyo, ndipo pamene adayamika, adagawira iwo akukhala pansu, momwemonso ndi tinsomba monga momwe iwo anafuna. Ndipo pamene adakhuta, Iye ananena kwa ophunzira ake: “Sonkhanitsani makombo. Kutu kasataike kanthu.”

— Yohane 6:11-12

Mu nkhani imeneyi, tikuona kutu anali Yesu amene anawauza kutu apite kukasonkhanitsa makombowo, kapena nyenyewazo, ndipo kutu kasataike kanthu. Ndikufuna inu mumvetse izi.

Anayenera kuwauza kuti achite zimenezo chifukwa sanaone mwayiwo. Dziikeni nokha mu malo mwawo. Mwadya kwambiri ndi kukhuta, ndipo chomwe mukufuna kuchita ndikupumula ndikugona. Chifukwa cha maphunziro anu a temberero la padziko lapansi ndi malingaliro anu aukapolo, pamene mwakhutitsidwa, imakhala nthawi yoti musiye. Mukuona, malingaliro aukapolo amagwira ntchito pokhapokha pamene ayenera, ndipo pamene sayenera, pamene akhutitsidwa, amasiya. Yesu anayenera kuwauza kuti asonkhanitse chimene chinali pamaso pawo. Makombowo anali panso ponse atawazungulira, koma sanayese kuatola. Koma tsopanonso mmaganizo mwawo, kodi makombowo anali amtengo wapatali motani osangowasiira mbalame?

Yesu anali kuyesa kuwaphunzitsa chinthu china chake chofunika kwambiri. Yesu akupereka ndemanga pambuyo powauza kuti asonkhanitse makombowo, kuti pasataike kanthu! Koma kodi zimenezi zikutanthauza chiyani? Aliyense wadya kwambiri, aliyense wakhuta, ndipo palibe amene akufuna mkate wina ndi nsomba zina, chabwino pakali pano. Koma vuto ndi ili—palibe mpumulo wa Sabata popanda kusonkhanitsa zambiri kuposa zimene mukufuna. Pamene Aisrayeli anatola mana pa tsiku la chisanu ndi chimodzi, anauzidwa kuti asonkhanitse mana kuposa mmene anafunikira. Kutolera koposa zimene anali kufuna pa tsikulo kunapangitsa kuti akhale ndi zofunika zawo zapa tsiku lachisanu ndi chiwiri, tsiku lopuma. Yesu anali kuphunzitsa ophunzira Ake kuti asaman-gokhutira ndi kuona zofunikira zonse za Ufumu. Apanso, simungathe kumanga ndi kukhutitsidwa, koma mukhoza kumanga ndi magawo awiri. Kukhutitsidwa ndi kudya mkate wa lero koma madengu khumi ndi awiri otsala amakupatsani zothandiza za mawa.

Nayi fundo yofunikira yomwe ndikufuna muone.

Ngakhale kuti ophunzirawo sanaone makombowo mpaka Yesu atawasonyeza, Mulungu **anali atawapatsa kale mpumulo wa Sabata**, magawo awiri. Iwo sanachione ichi. Ufumu unali utapereka kale chakudya, kuchulukitsa mkate ndi nsomba, ndi kudyetsa anthu onsewo—koma Ufumu nthawi zonse umapereka magawo awiri. Mulungu sadzangopereka kukhutitsa; **Nthawi zonse Adzapereka zokwanira koposa**. Vuto ndiloti mwina simukuziona!

Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwa inu. Muyeso wabwino, wotsendereka, wokhuchumuka, wosefukira, ndipo adzakupatsani mmanja mwanu. Pakuti kudzayesedwa kwa inu ndi muyeso womwewo, muyesa nawo inu.

— Luka 6:38

Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwa inu, muyeso wabwino, wotsendereka, wokhutchumuka. Koma apa sipamene ndimeyi ikuimira. Muyeso wanu wotsendereka, wokhuchumuka ndizo zofunika zanu za tsiku limenelo. Koma ndimeyo ikupitiriza kunena kuti, “ndi kusefukira!” Kusefukira ndi magawo awiri. Mulungu nthawi zonse amapereka magawo awiri, osati okwanira okha!!!! Koma ngati simunadziwe za ichi, kuti njere ikusefukira, mutha kungoisiya kuti igwe pansi pamene mutayang’ana gawo lokhutitsidwa lomwe lili patsogolo panu ndipo mosakonzekera mulandira kusefukira kwake. Potero, mungalephere kugwira ndi kusangalala ndi magawo awiri. Koma ngati mudakazindikira mmene Ufumuwo ukugwirira ntchito, ndikudziwa ndi kuyembekezera zofunikira zonse, mudakakhala wokonzekera kuchitapo kanthu ndi kulandira zonse zimene Mulungu amapereka.

Ndiloreni ndikupatseni chitsanzo china.

Ndipo Simoni anayankha, nati, “Ambuye, tinagwiritsa ntchito usiku wonse osakola kanthu. Koma pa mawu Anu, ndidzaponya makoka.” Ndipo pamene anachita ichi, anazinga unyinjira wa nsomba ndipo makoka awo anali kung’ambika. Ndipo anakodola anzawo a mngalawa inayo adze awathangate, ndipo anadza nadzadza ngalawa zonse ziwiri motero kuti zinali nkumira. Koma Simoni Petro pamene anaona, anagwada pa mabondo ake a Yesu nanena, “Muchoke kwa ine, Ambuye; chifukwa ndine munthu wochimwa!” Pakuti chizizwo chidagwira iye ndi onse amene anali naye pa kusodzako kwa nsomba zimene anazikola, ndipo chimodzimodzinso Yakobo ndi Yohane, ana a Zebedayo, amene anali anzake a Simoni.

— Luka 5:5-10

Ili ndi gawo la nkhani yomwe tawerenga kale. Petro anali ndi ngalawa ziwiri zimene zinatsala pang’ono kumira ndi nsomba chifukwa cha Ufumu. Ichi chinali chosiyana ndi kamvedwe kake ka kusodza ndipo zinamudabwitsa. Koma ndi chiani chinachitika chotsatira pamene Yesu ananena kuti: “Petro, pita uko ku madzi akuya, ndipo udzagwira nsomba zochuluka monga mmene ungasungire?” Kodi mukuganiza kuti akanatenga ngalawa ziwiri? Ndikukaika. Iye akanankhanitsa ngalawa zambiri zomwe akanabw-ereka kwa anzake. Chifukwa chiyani? Chifukwa chakuti iye anali ndi chiyembekezo chosiyana ndi chidziwitso cha mmene Ufumu umagwirira ntchito.

Cholinga cha zokambirana zonsezi ndikuti muonetsetse pamene simukumvetsetsa pa zofunikira zomwe Mulungu akutumiza. Zoonadi, nthawi zambiri zofunikirazo sizikhala ngati ndarama zolipirira zinthu. Koma zidzakhala mu maonekedwe a malingaliro,

kuikidwa kwaumulungu, ndi chitsogozo cha Mzimu Woyera. Ngati sitinakonzekere ndi kumvetsetsa koyenera za magawo awiri, tidzayenda pafupi ndi iwo chifukwa cha maphunziro athu a kupulumuka pa dongosolo la temberero la dziko lapansi.

Mu nkhani ya kuchuluka kwa mkate, Yesu akuyesetsa kuphunzitsa ophunzira Ake mmene Ufumu umagwirira ntchito, zimene ayenera kuyembekezera komanso zimene ziyenera kuchitika. Chifukwa chakuti malingaliro awo a ukapolo sanali kuona kufunikira kwa mkate wonsewo unali pansu, Iye anayenera kuwaphunzitsa kuti ayang'ane: “Mukuona chiyani?”

Taonani! Inu simukuonazonse zimene Mulungu wakukonzerani.”

Ndikufuna ndikukumbutseni za Eksodo 16 kwa kamphindi popeza pali chinthu chinanso chomwe ndikufuna kunena.

Ndipo anauola mmawa ndi mmawa yense monga mwa njala yake, popeza likatentha dzuwa, umasungunuka. Ndipo kunali tsiku lachisanu ndi chimodzi, anaola mkati nawon-jezapo linzake—maomeri awiri pa munthu mmodzi—ndipo akazembe a khamu anadza nauza Mose. Ndipo ananena nawo: “Ichi ndi chomwe Yehova analankhula: ‘Mawa ndiko kupuma, Sabata lopatulika la Yehova. Chimene muziotcha otchani ndi chimene muziphika phikani. Ndi chotsala chikukhalireni chosungika kufikira mmawa.’”

Ndipo anausunga kufikira mmawa, monga adalamulira Mose, koma sunanunkha ndipo sunagwa mphutsi. Ndipo Mose anati, “Muudye lero, pakuti lero ndilo Sabata la Yehova; simuupeza lero pabwalo. Muziwola uwu masiku asanu ndi limodzi, koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo la Sabata; pamenepo padzakhala palibe.”

Ndipo kunali, tsiku la Sabata kuti anthu ena anatuluka kukawola, koma sanaupeze. Ndipo Yehova anati kwa Mose: “Mukana kusunga zouza zanga ndi malamulo anga kufikira liti? Taonani popeza Yehova anakupatsani Sabata; chifukwa chake tsiku lachisanu ndi chimodzi ali kupatsa inu mkate wofikira masiku awiri. Khalani yense mmalo mwake; munthu asatuluke mmalo mwake tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Ndipo anthu anapumula tsiku lachisanu ndi chiwiri.”

— Eksodo 16:21-30 (mana)

Monga takhala tikunena, magawo awiri ndi omwe adapangitsa mpumulo wa Sabata kukhala wotheke. Koma chodabwitsa ndi chakuti, ngakhale kuti Mulungu anali atapereka kale magawo awiri pa tsiku lachisanu ndi chimodzi, ambiri a iwo anapita kukawafunafuna koma sanawapeze pa tsiku la sabata. Sikuti Mulungu sanali wokhulupirika kuwapatsa. Iwo sanachione chifukwa chakuti sanamvetsetse bwino za magawo awiri amene anaperekedwa kale pa tsiku lachisanu ndi chimodzi. Anali atasonkhanitsa okwanira tsiku limodzi lokha, monga mwa masiku onse. Tsopano popeza anali ndi njala pa tsiku la chisanu ndi chiwiri, sanapeze chilichonse. Mwina mmaonedwe awo Mulungu adawalepheretsa. Koma Mulungu sanalephere; iwowa sanali kudziwa za fundo ya magawo awiri. Akadadziwa, akanakonzekera mosiyana.

Ndi anthu angati masiku ano amene akungoyendayenda pofuna kupeza zimene akufuna, osadziwa kuti Mulungu wazitumiza kale? Ndikuganiza kuti ndizosangalatsa kwambiri mu ndimeyi kuti Mulungu wawakwiira chifukwa chosasonkhanitsa zokwanira!!!! Ine ndikudabwa momwe izi zikhoza kulalikiridwa mu mipingo yathu.

Ndipo iye wakupatsa mbewu kwa wofesa, ndi mkate ukhale chakudya, adzapatsa, ndi kuchulukitsa mbewu yanu yofewa, nadzaonjezapo pa zipatso za chilungamo chanu. Polemeretsedwa inu mzonse ku kuwolowa manja konse.

— 2 Akorinto 9:10-11

Paulo akunena momveka bwino pano pamene akufotokoza zotsatira za Ufumu wa Mulungu kuti umakhala wolemeretsa inu mzonse ku kuwolowa manja konse. Mnzanga, izi zimafuna magawo awiri. Simungathe kukhala owolowa manja nthawi zonse popanda zokwanira zoposa.

Mmutu woyambirira, ndidagawana nanu momwe malonda yanga adayendera kuchokera ku 3 mpaka 4 *million* pa mlingo wazopangidwa pa chaka ndi mmodzi wa otigula kupitirira ku 11 *million* pachaka ndi wa wotigula yemweyo. Kuwonjezeka konseku kunachitika mu chaka chimodzi chokha. Ndinakuuzaninso mmene zimenezi zinachitikira, kuti Mulungu anandipatsa loto usiku ndikundiuzana mmene ndingachitire. Koma tsopano ndiyenera kukuuzani zimene anandiuzana chifukwa tsopano zidzamveka kwa inu. Mu maloto anga, Iye anangondipatsa mawu awiri. Inde, mawu awiri okha. Mawu awiriwa adasintha ndarama zomwe ndimapeza ndi mazanamazana chaka chimenecho popanda ine kunenerera kapena kutsatsa kuposa momwe ndimachitira kale. Palibe chimene ndinasintha chokhudza ntchito ya *company* yanga kupatula ine. Mawu awiri amenewo anandipatsa malangizo oti ndisinthe mmene ndinali kuchitira zinthu, ndipo kusintha kumeneku kunachulukitsa kowirikiza kanayi malonda athu ndi ndarama zomwe ndimapeza. “Mawu awiriwa ndi chiyani?” mukufunsa. Chidule chake ndi ichi—Likaomba Wotheratu!

Inde, likaomba wotheratu. “Ndichoncho? Mawu awiri aja

adachita zonsezi?” Inde, iwo anatero. Mukamvetsetsa kuti Mulungu NTHAWI ZONSE amatumiza magawo awiri ndi zofunika Zake, mudzamvetsetsa zomwe Anandiuza.

Company yanga, monga ma *company* onse ogulitsa, imapanga phindu pothandiza anthu. *Company* ikakhala yabwino ndikuthandiza anthu, ndarama zambiri zimapangidwa. Ngakhale izi ndi zoona, ndizoonanso kuti ma*company* ambiri ogulitsa amalephera kukwan-iritsa zosowa za owagula mwina chifukwa chosawatsata bwino komanso chisamaliro cha owagula kapena kusowa kulondola ndi kupeza owagula atsopano a *company* imeneyo.

Kwa ife, tinali otanganidwa kwambiri, ndipo ngakhale kuti sichinali chinthu choipa, nthawi zina sitinali kupereka nthawi yambiri yomwe ndikadakonda kuona otigula. Kwa ine ndekha, ndimagwira ntchito ndi otigula oikiza ndarama zawo ndipo ndimazikonda. Koma

**AMBUYE AMANDIUA
KUTI KUSEFUKIRA,
MPUMULO WA SABATA,
UNALI KALE PAMENEPO,
IYE ANALI ATAUPEREKA
KALE. SINDINALI
KUUONA CHABE!**

chifukwa cha dongosolo langa, pamene wofuna kugulitsa ndarama aimba ndipo apatsidwa kwa ine kuti ndimuthandize, nthawi zina sindimuimbiranso mmaola 24 oyambirira. Zolinga zanga ndi zabwino koma sizichitika.

Monga mukudziwa, pamene anthu afunsa mafunso, *company* yomwe imapereka mayankho ndi yomwe imapeza malonda. Nthawi zina kuchedwetsa kuimbira ogula kuti akambirane zakuikiza ndarama zawo zitha kukhala zochedwetsa kwambiri. Iwo akadatha kuimbira munthu wina amene analipo kuti ayankhe mafunso awo. Pali zinthu zambiri zomwe zingasokonekere, koma yankho ndilakuti pazikhala munthu wopereka mayankho pamene anthu akufuna kudziwa.

Chotero pamene Ambuye anandipatsa mawu awiri amenewo, ndinadziwa tanthauzo lake. Ndinayenera kuyang'ana zinthu mosiyana ngati ndikanakhaladi pa nsanja imeneyo, mu gulu la anthu khumi apamwamba ndikulandira bonasi ya \$100,000. Ndinayenera kutenga nthawi! Choncho ndinasintha mmene ndinali kuchitira zinthu. Ndinaika lamulo lakuti ngati aliyense wabwera kudzandifunsa za ndarama, ndimuimbirensa mmphindi zingapo zitapita, ngati nkotheke, ndiwachezere mwamsanga. Amalonda anga ali mdziko lonselo ndipo kudzipereka uku kunali kovuta kuchita. Koma ndinadzipereka ku ichi. Ndinaitana woyang'anira *company* yanga ndi kumuuzza zimene Mulungu ananena kuti auze oimira anga onse kukhala ndi maganizo ofananawa ogwiritsira ntchito mpata uliwonse ukakhalapo. Chaka chitatha, tinachita zoposa 11 *million* zomwe zidatiyenereza kukhala mu gulu la khumi apamwamba kwa wa malonda ameneyo. Koma pamwamba pa izi, tinali titapezanso malonda owonjezera ma *million* kwa malonda athu ena.

Nayi nthawi yaikulu yonena zobisika. Sitinachite chosiyana koma tinangochitapo kanthu mwamsanga pamene tinakhala ndi wotigula amene anafuna kutilankhula. Mukuona, Ambuye amandiuza kuti kusefukira, mpumulo wa Sabata, unali kale pamenepo, Iye anali ataupereka kale. Sindinali kuuona chabe!

Chotero palibe lamulo la magawo awiri mu Ufumu limene linakhazikitsidwa. Gawo lachiwiri likhala lilipo nthawi zonse. Mulungu amapereka nthawi zonse pamlingo wa magawo awiri.

MULUNGU SATUMIZA ZOFUNIKIRA KWA LERO LOKHA. NTHAWI ZONSE AMATUMIZA MAGAWO AWIRI NDI IZI!

Apanso, vuto lathu ndikuti sitikuona magawo awiri.

Koma vuto lalikulu ndilakuti sitinadziwe ngakhale kuwayang'ana!!!!

Ndimakonda zomwe Yesu ananena, “Kuti kasataike kanthu!” Mulungu anatumiza izo zonse, ndipo Iye akufuna kuti inu mukhale nazo. Iye anakhumudwa kuti anthu anali kunjakuafuna mana pa tsiku la chisanu ndi chiwiri pamene Iye anali atawatumizira kale. Iye anakumbutsa Mose kuti anatumiza pa tsiku lachisanu ndi chimodzi kuti akapeze ndi kusangalala ndi mpumulo wa Sabata. Kwenikweni, anali kuwauza kuti, “Sabata si langa, koma ndi lanu. Ndi chifukwa chake ndakutumizirani magawo awiri.” Inu mukhoza pafupifupi kumva Yesu akunena chinthu chomwecho. “Eya anyamata, nyamulani makombowo, ndipo mutenge onse. Mulungu anawatumizira kuti mutenge, kuti musangalale ndi magawo awiri ndi kupeza mpumulo.”

Mu nkhani ya Yesu yodyetsa anthu zikwi zisanu ndi mikate isanu ndi nsomba ziwiri, ophunzirawo sanaone makombo. Iwo sanali kuwafunafuna ayi. Koma Yesu anawauza zoti atole ndipo zofunikirazo sizinatsale. Lero Mzimu Woyera uyenera kutithandiza kuona kukhutitsidwa kale ndi kutenga magawo awiri. Adzalozera kwa ife zinthu zomwe sitikuziona ngati tidzamufunse. Fundo yomwe ndikuyembekeza kuti mwaphunzira mpaka pano ndikuti magawo awiri aperekedwa kale kwa inu; kumangofunika kuti muwatole.

Chifukwa chakuti magawo awiriwo ndiwo njira YOKHAYO yothawira dongosolo la temberero la pa dziko lapansi la ntchito yowawa ndiyokukhetsa thukuta, Satana amadana nayo. A-aa, iye akhoza kuyesa kukhutitsa Akristu kuti ngati akulipira ngongole

zawo, kugwira ntchito ziwiri kuti asungike, akuchita zonse bwino. Koma Mkristu amene ali ndi ndarama zothandiza Ufumu wa Mulungu ndipo akukhala moyo wopanda mantha andarama ndi nkhwana—tsopano ameneyo ndiye amene amafuna kumusiya. Cholinga cha satana ndikukupangitsani kukhala wosowa masiku onse amoyo wanu ndikukuikani mu ukapolo wa moyo wofuna kungopulumuka kumene mulibe nako mphamvu. Ndarama ndi mphamvu! Satana angakonde kwambiri kukuletsani ku madalitso a Mulungu. Ndiye chifukwa chake zomwe ndikufuna kukuuzani ndizofunikira kwambiri kuti mumvetsetse.

Gawo lachiwiri ndi lobisika!

Chabwino, ndi nthawi yakupumula kwa ophunzira Ake. Panali chifukwa chomwe sanaonere kusefukira. Inde, monga takhala tikunenera, iwo sanali kuyang’ana, koma panali chinthu china kwenikweni. Nthawi zambiri simutola zotsalira! Ndikutanthauza kuti, mmaganizo mwawo, mkate ndi timagawogawo ta nsomba tomwe tinali panso pozungulira tinali totsallira chabe.

Ndi chifukwa chiani ndarama imene Petro anafunikira kuti apereke msonkho inabisidwa mkamwa mwa nsomba? Ndani angaganize konse kuyang’ana mmenemo? Ndani akadaganiza kuti ngalawa ziwiri za asodzi odziwa bwino ntchito amene anasodza usiku wonse osagwira kanthu kuti angakhoze kugwira nsomba zambirimbi za pa miyoyo yawo ndi mawu a Rabi? Ndani akadaganiza kuti mkazi wa ku 2 Mafumu 4 yemwe analibe ndarama, alibe kanthu mnyumba mwake koma mafuta pang’ono, ndipo anali pafupi kutsimikiza kuti alibiretu ndarama ndipo mwina kuti anali ndi mafuta okwanira kuti analipira ngongole ndi kumlola

kukhala moyo womasuka? Palibe adanatero. Ndani akadaganiza kuti Gary Keese, amene anachoka mu umphawi, ndikukhala *millionaire* lero ndikumalankhula ndi zikwi za anthu kuzungulira dziko lapansi

**CHOLINGA CHA SATANA
NDIKUKUPANGITSANI
KUKHALA WOSOWA
MASIKU ONSE AMOYO
WANU NDIKUKUIKANI
MU UKAPOLO WA MOYO
WOFUNA KUNGOPULUMUKA
KUMENE MULIBE NAKO
MPHAMVU.**

tsiku ndi tsiku? Palibe ndi mmodzi yemwe! Mu nkhani zonsezi, Mulungu anagwiritsa ntchito zosayembekezereka kusintha zinthu.

Ngati kusefukira, kwa magawo awiriwo kunali kodziwikiratu, poyera, Satana akadaona ndipo akadayesera kuwaletsa ndi kuwaba. Ndichifukwa chake Mulungu saulula chuma Chake poyera. Icho ndichobisika. Satana amadana ndi inu kuti mukhale okhutitsidwa ndi kusangalala ndi

zofunikira, koma kwenikweni amadana nazo ngati mutalowa mu kusefukira ndi mpumulo wa Sabata.

Ndiloreni ndikusonyezeni china chake chimene muyenera kuchimvetsa ponena za mmene Mulungu amagwirira ntchito padziko lapansi.

Koma, tilankhula nzeru ya Mulungu m'chinsinsi, yobisikayo imene Mulungu anaikiratu pasanakhale nyengo ya pansi pano ku ulemelero wathu. Imene saidziwa mmodzi wa akulu a a nthawi ya pansi pano, pakuti akadaidziwa, sakadapachika Ambuye wa ulemerero.

— 1 Akorinto 2:7-8

Ndimeyi ikutionetsa momveka bwino kuti Satana akadadziwa dongosolo la Mulungu, akadasintha machenjerero ake! Ichi ndichifukwa chake Mulungu ayenera kugwira ntchito mobisa. Satana akhoza kuchita pa chilichonse chodziwikiratu. Kuchuluka kwa zofunikira zanu sikungadziwike poyera mpaka nthawi yomwe mudzatole kapena kukolola. Ndili ndi mwambi womwe ndakhala ndikunena kwa zaka zambiri. Chuma cha Mulungu ndi chobisika, osati kwa inu koma cha inu.

Chabisika *kwa inu cha inu!*

Anthu ambiri amandiuza kuti akufuna kuti Mulungu asadikire mpaka potsirizira penipeni kuti abweretse mayankho Ake. Koma bwenzi langa, Mulungu sapupuluma. Amadziwa nthawi yolipira ngongoleyo, ndipo ndi phindu kwa inu kuti Mulungu asaonetse dzanja Lake mofulumirirapo kuopera kuti Satana angawatsekereze.

Ndipo ndidzakupatsa iwe chuma cha mundima, ndi zolemera zobisika za m'malo a m'tseri, kuti iwe udziwe kuti ine ndine Yehova, amene ndikuitana iwe ndi dzina lako, ndine Mulungu wa Israyeli.

— Yesaya 45:3

Zolemera zobisika za m'malo a m'tseri? Eya, izi ndizabwino kuposa zolemba zazikulu kwambiri za kanema waku Hollywood. Ndiloreni ndikupatseni chitsanzo cha momwe Mulungu adandithandizira kutola magawo awiri mu moyo wamalonda anga. Zaka zapitazo, ndinakhala pansu ndikuyang'ana lipoti la ndarama langa

la pachaka la *company* yanga ya za ndarama. Ngakhale kuti ndinali wokhutitsidwa—ndinalibe ngongole ndipo ndinali ndi ndarama zina kunkhokwe ya ndarama—ndinadziwa kuti panalinso zina. Ndinaona ntchito zambiri zimene ndinali kufuna kuti ndithandize mu Ufumu, zambiri, ndipo zonse zimafunika ndarama.

Pamene ndinapemphera za ichi, Ambuye anayamba kuchita nane za mawu a *makombo*. Poyamba sindinali kumvetsa zomwe Anali kunena. Koma pamene ndinapemphera kwa nthawi yaitali za ichi ndi kumvetsera, ndinachidziwa. Makombo monga mu nkhani imene tangowerengayi ananyalanyazidwa. Kufunika kwawo kunali kuonedwa ngati kopanda pake— mwina chifukwa cha mphamvu zofunika powatolera poonedwa kuti ndi osayenera kapena kuti kufunika kwake kunali kokhazikika pa dongosolo lachikale. Kapenanso, malingaliro olakwika ndi ochepera a momwe angagwiritsire ntchito amalepheretsa kumvetsetsa kwawo kwa kuchuluka ndi kufunika kotengera momwe kunali kuonekera nthawi imeneyo.

Ndikutsimikiza kuti mwamvapo anthu akunena ichi nthawi zambiri, “Umu ndi momwe timachitira nthawi zonse.” Chabwino, ndikuuzeni kuti magawo awiriwo mwina sangabwere mwanjira imeneyo.

Pamene ndimayang’ana lipotili, Mulungu anatsegula maso anga ku makombo ambiri omwe ndinali kuwasiya patebulo zomwe ndimayenera kuzitolera. Chimodzi mwazinthu zofunika kwambiri zomwe timachita ndi wotigula aliyense ndikulemba mbiri yawo yonse kuti tione zinthu zomwe angakhale nazo komanso ngongole zawo. Kenako timasanthula kuti tiyang’ane ndarama zilizonse zomwe tingathe kukhala nazo pakubweza ngongole. Zachidziwikire, timalemba zomwe ali nazo pa nthawiyo ndi chiwongola dzanja chake, kuphatikiza malamulo obwerekera. Panthawiyo,

takhala tikulangizanso otigula kuti apeze ngongole yanyumba polinganiza ndi zimene ali nazo mnyumba kuti asalipire chiwongola dzanja chachikulu, motero timachepetsa chiwongola dzanja chawo kuchoka pa 21% kufika pa 6% pamtengowo. Ndarama zotsala pa izi zidapulumutsa banja wamba limene limapeza \$500 mpaka \$600 pamwezi. Izi zikachitika, timatumiza otigula kumankhokwe awo a ndarama kuti akapeze ngongole yophatikiza.

Pamene ndinali kuphunzira za lipoti langa, Mzimu Woyera anandilozera za nkhani yogulitsa nyumba. “Bwanji osagwira ntchito ya zogulitsa nyumba?” Pamene ndinaganizira za ichi, zinali zomveka. Tinali kale ndi chidaliro cha otigula; tinali ndi lipoti yake kale; ndipo pomalizira pake, ndife amene tinali kunena kuti akonzenso ngongole zawo poyamba.

Kuti ndigwire mbali iyi yamalonda kukadafuna ine kuti ndiphunzire malonda yatsopano, ndipambane maphunziro a makalasi opatsa chilolezo, ndi zina zambiri. Ndinalibe nthawi yochitira zonsezi. Koma pamene ndinapitiriza kupempherera ichi, Yehova anandilimbikitsa kulemba munthu wina wa ganyu woti akhazikitse ndi kuyendetsa *company* yanga yogulitsa nyumba, ndi chimene ndinachitadi. Kugwira ntchito yogulitsa tokha mu chaka choyamba chokhacho kunabweretsa ndarama zowonjezera \$160,000 mu ndarama zolowa zonse. Izi zinali ndarama zomwe sindikadakhala nazo ndikadapanda kulola Mzimu Woyera kuloza makombo ndinali kuwayang’ana koma osawaona.

Ndinapitiriza kugwira zinthu zina zambiri zomwe zinali makombo omwe Mzimu Woyera anandionetsa. Kombo limodzi imene ndinali kuyinyalanyaza—chifukwa cha malingaliro anga odziwika kale amene ndinaphunzira kapena kumva kwa anthu ena akunena kuti mbali imeneyi sinali yofunika kulowamo—inakhala

chipambano chachikulu kwa ife. Nditakhala pansi potsirizira ndikuiyang'ana, ndinazindikira kuti zonse zomwe ndinamva zokhudza malowa zinali zolakwika ndipo zinali zoyenera kwambiri ku *company* yathu. Makombowa atulutsa ndarama zambiri zolowa kuposa momwe malonda yanga akulu alili, kubweretsa mamillion a madola. Analidi makombo a madola mamillion ambiri!

Choncho ndiloreni ndikufotokozereni momveka bwino. Magawo awiri anatoledwa kudzera mu vumbulutso! Vumbulutso ndi chinthu chomwe Mzimu Woyera akukuonetsani chomwe simukanachidziwa mwa inu nokha. Kotero Mzimu Woyera umavumbulutsa kapena kutsegula maso anu ku china chake chimene mwa inu nokha simukanachidziwe. Ichi chimatchedwa chidziwitso cha vumbulutso.

Vumbulutso ndilo fungulo ku magawo awiri!

Kenako anthu amandifunsa kuti, “Kodi ndimaumva bwanji Mzimu Woyera? Kodi ndimamva bwanji momwe ndingatolere zobisika izi malingaliro ndi mwayi?” Mafunso abwino. Ndilibenenthawi mu bukuli kuti ndifotokoze mozama za kumva liwu la Mulungu. Choncho ndikulozereni ku buku lina limene ndalembe lotchedwa, *The Baptism of the Holy Spirit* (Ubatizo wa Mzimu Woyera.) Mutha kugula kudzera ku Amazon kapena patsambalathu. Mu buku limenelo, mudzapeza zambiri zokhudza mmene Mzimu Woyera umagwirira ntchito kuulula zolinga zobisika za Mulungu kwa ife, kuti titha kuchita bwino pompano padziko lapansi, pamaso pa Satana; ndipo palibe chimene angachite. Koma kuti mupite mu njira yoyenera, tiyeni tione pa **1 Akorinto 14:2**.

Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu koma ndi Mulungu. Pakuti, palibe munthu wakumva; koma mu mzimu alankhula zinsinsi.

Ndime 4 imati,

Iye wolankhula lilime adzimangirira yekha.

Liwu loti kumangirira limatanthauza kubweretsa malangizo kapena kumvetsetsa. Ndikufuna chimenezo ndipo inunso. Pamene Baibulo likulankhula pano za kulankhula malilime kapena, monga Paulo akulongosolera, kupemphera mu Mzimu, ine ndikufuna kuti ndikulimbikitseni inu—zilibe kanthu zomwe mwamva za ntchito iyi ya Mzimu Woyera, kaya wina wakuuzani kuti inalekeka ndi atumwi kapena kuti ndi ya mdierekezi—werengani Baibulo lanu! Kupemphera mu Mzimu ndi kuti Mzimu Woyera amapemphera kudzera mwa inu padziko lapansi kuti chifuniro Chake chichitike popanda mdierekezi kudziwa zomwe zikuchitika. Kupemphera mu Mzimu ndi fungulo lalikulu pakumva vumbulutso lochokera kumwamba, ndipo ndikukulimbikitsani kuti muphunzire zomwe ndanena. Ndipo ngati muli ndi mafunso, pezani buku langa ndipo ndikudziwa kuti likuthandizani kudziwa zambiri zozama za ntchito yodabwitsa ya Mzimu Woyera mu miyoyo yathu.

Ndikufuna kumalizitsa bukuli ndi ndime ziwiri za m'Malembu omwe akufotokoza mwachidule mutuwu.

Ndipo kwa Iye amene angathe kuchita kopoulosatu zonse zimene tizipempha kapena tiziganiza, monga mwa mphamvu yakuchita mwa ife, kwa Iye kukhale ulemmero mu mpingo

ndi mwa Kristu Yesu kufikira mibadwo yonse ya nthawi za nthawi! Amen.

— Aefeso 3:20-21

Simungathe kupempha chinthu chomwe simunachiganizire. Panopa ndili ndi ndege ziwiri, ndege yaing'ono yomwe ndimayenda mongosangalala chabe komanso ndege yanga yamalonda yomwe ndimayenda nawo kulikonse kudziko komwe ndikupita. Pamene ndinali kuganiza zogula ndege yochitira malonda, ndinadabwa kwambiri ndi mtengo wake. Ndege sizitsika mtengo! Ndinayamba kubwerera kumbuyo ndikuganiza, “Ndingathe kuchita popanda ndege yamalonda. Pajatu ndi ndarama zambiri.” Koma ndinali kuyenda pandege mlungu uliwonse pa ndege ya zamalonda, ndipo mwezi wina ndinauluka maulendo makumi awiri mphambu zitatu. Zinali zotopetsa. Inde, ndikhoza kunena kuti ndinali ndi zofunikira. Maulendo anga onse adalipiridwa; panalibe zovuta ndi ndarama zolipira. Koma ma ulendo wanga a pandege anakhala chinthu koma chopereka mpumulo. Ulendo wa pandege ukaimitsidwa kapena ukachedwetsedwa, zinali zovuta. Uwu sunali mpumulo wa Sabata umene ndimafuna.

Potsirizira pake, ndinavomereza kuti ndikuika malire kwa Mulungu pano. Iye ndiye Mulungu wa magawo awiri. Pepani kuti ine ndi Drenda tinakaikira kugula ndegeyo kwa chaka chimodzi. Pomalizira pake, Mulungu analandira chidwi chatu pa ndegeyo ndipo anatiuza kuti Wakhala akuyesera kutipezera ndegeyo kwa zaka ziwiri! Tinalapa ndi kuchita chitsimikizo chatu. Tinafesa mbewu zathu za ndege yamalonda yeniyeni yomwe tinali kufuna; ndipo pamene tinatero, tinali nayo mkati mwa miyezi iwiri. Panthawiyi, Mulungu anandipatsa luntha ndi chiyanjo ndi malonda ena, ndipo ndaramazo zinalipo pamene ndinazifuna.

Inde, Mulungu ndi Mulungu wa magawo awiri. Kodi zinasintha? Chabwino, kusiyana m'moyo wanga wokhoza kuwuluka ndege yangayanga poyerekeza ndi kuwuluka pa ndege yolipira kungakhale ngati kuyerekeza kukwera njinga yanu kapena kuyendetsa galimoto kupita ku msonkhano pa mtunda wa mailoai makumi asanu. Zoonadi! Ndipo Mulungu anali kuyesera kuti aifikitse izo kwa ine kwa zaka ziwiri pamene ine ndinali kungoyang'ana pa kukhutit-sidwa ndi kukhala wakhungu ku magawo awiri omwe Mulungu anali atandipatsa kale. Ndinali kungofuna kuziona.

Mwina mukhoza kukhala mukuyendetsa galimoto yomwe ikufunika kukonzedwa kotero kuti mumapemphera kuti ilire mukadzuka. Lekani kuyang'ana ku nkhekwe yanu ya ndarama yopanda kanthu ndikupanga zitsimikizo zopulumukira pa izo. Mmalowake, lolani Mulungu wa magawo awiri akusonyezeni makombo, zinthu zobisika zimene muyenera kuzidziwa kuti mukhale mfulu ndi kusangalala ndi mtendere ndi mpumulo wa Sabata. Adzakupatsani dongosolo ndi kukuonetsani momwe mungachitire ngati mungomupempha Iye. Monga mmene Yesu ananenera, “Kuti kasataike kanthu!” Magawo awiri aperekedwa kale kwa inu!

Momwemo utatsalira mpumulo wa Sabata wa kwa anthu a Mulungu. Pakuti iye amene adalowa mpumulo wake, adapumulanso mwini wake ku ntchito zake monganso Mulungu ku zake za Iye.

— Aheberi 4:9-10

Ndikukhulupirira kuti buku ili lakhala dalitso kwa inu ndi kuyenda kwanu ndi Ambuye Yesu Kristu. Monga ndidanenera mu bukuli, ili ndi lachiwiri pamndandanda wa “Kusinthika Kwa Chima Chanu.” Onse pamodzi adzakhala okwana asanu, choncho pitirizani kudikirira buku lotsatira pa *website* yathu. Komanso, lingalirani kukhala chiwalo cha *Team Revolution*, dongosolo lathu lophunzitsira. Muthanso kudziwa zambiri za *Team Revolution* patsamba lathu.

Gary ndi Drenda Keesee ndiwo eni ake ndi ogwira ntchito ku Forward Financial Group ku New Albany, Ohio, 1-(800)-815-0818.

Gary ndi Drenda Keesee ndi abusa a Faith Life Church ku New Albany, Ohio.

Kuti mudziwe zambiri za Gary ndi Drenda Keesee, pitani ku Faith-LifeNow.com, GaryKeesee.com, kapena ku Drenda.com.

Pita ku **FLNFree.com**
kukatenga maphunziro ena aulere
m'chilankhulidwe chako!

Ukufuna zipangizo za mphunziro AULERE m'chilankhuliwe chako?
Pita ku **Free.com**

KUSINTHIKA KWA CHUMA CHANU

Mphamvu ya Mpumulo

Kodi mwatopa?

Kutopa ndi mpikisano wopezera chuma?

Kutopa ndi kumva kupanikizika?

Kutopa ndi kudandaula?

Kutopa ndi kusasangalala?

Simuyenera kukhalanso moyo wotero.

Phatikanani ndi Gary Keesee paulendo wake wodabwitsa wakuzindikira, ndi KUPHUNZIRA DONGOSOLO LATSOPANO—limodzi limene lidzasinthiratu moyo wanu, monga mmene linachitira wake patapita zaka zisanu mphambu zinayi za kukhala *wotopa* komanso kusowa pogwira pa zachuma, zathupi ndi zapamalingaliro.

Fufuzani:

1. Mmene zonse zinasinthira kwa Gary—momwe anasinthira kuchoka pakukhala wosowa chuma ndi kuthupi, ku kukhala wathanzi komanso wodzala, kulipira ndalama zonse pogula magalimoto, kumanga nyumba yake popanda ngongole, kuyambitsa ma *company* angapo, ndikuphunzitsa anthu zikwi mazanamazana za moyo wa Ufumu ... za kukhala moyo wa mpumulo.
2. Momwe chilichonse chingasinthire kwa INU, inunso—mmene mungakhalire moyo wa mpumulo.

Ngakhale kuti aliyense amene mukumudziwa akukhala wotopa komanso akuthamangathamanga kuti apulumuke, simuyenera kukhala ndi moyo wotero.

Mwa kumvetsa mfundo yaikulu ya mpumulo wa Sabata, mutha kuona zotsatira zenizeni m'moyo wanu. Mutha kukhala pamalo omwe zosowa zanu zimakwaniritsidwa; wopanda mpikisano wopezera chuma; womasuka kupeza ndi kuchita bwino mu cholinga chanu ndi chikhumbo chanu, kumene mukuchita bwino kuposa kungopulumuka; ndi komwe mukuonetsa zotsatira zake kudziko kuti ndinu osiyana ndi zomwe amaona nthawi zonse.

Musakhale opanikizika. Musapitilire kukhala ndi moyo wotopa.

Pezani njira yatsopano yokhalira!



Gary Keesee ndi wolemba, wolalikira, wazamalonda, katswiri wa zachuma, ndi mbusa yemwe ali ndi chidwi chofuna kuthandiza anthu kupambana m'moyo, makamaka pankhani ya chikhulupiriro, banja, ndi zachuma. Gary ndi mkazi wake, Drenda, apanga malonda angapo opambana, ndipo ndi amene anayambitsa *Faith Life Now*, yomwe imapanga maprogram awiri apa television—*Fixing the Money Thing* ndi *Drenda*, misonkhano yapadziko lonse lapansi, ndi zipangizo zothandizira. Banja la a Keesee ndiwonso abusa a *Faith Life Church* imene ili pafupi ndi Columbus, Ohio.

P.O. Box 779, New Albany,
OH 43054, USA
garykeesee.com

Ukufuna zipangizo za mphunziro AULERE
m'chilankhuliwe chako?
Pita ku **FLNFree.com**